## KAWUNIWUNI WA CHIPANGANO CHATSOPANO (New Testament)

Panapita zaka 400 Mulungu asanayankhulenso kwa anthu ake. Nyengo imeneyi imatchedwa pakatikati pa zipangano monga chipangano cha sopano ndi chipangano cha kale. Pamene Baibulo lakhala chete osanena zochitika panthawiyi, Mbiri imalongosola zochitika zosiyanasiyana munyengoyi. Aperisi ndi omwe anali amphavu kumathero kwa chipangano chakale. Alekizanda mfumu yaikuluyo amene anali waku Gilisi anakhala olamula waderali. Anasogolera dziko la Gilisi kukhala lamphavu pa dziko lonse lapansi mosogozana ndi Aroma amene analibe amphavu kufikila pamene chipangano chatsopano chimayambika. Tiyeni tione mwachidule Mbiri ya ana a Mulungu kuchokera pa mfumu Solomoni kufikira kuchipangano chatsopano.

1. Ufumu wa kumpoto unatha pakati pa zaka za m'ma 930 mpaka 722 BC. Unakhala kwa zaka 208. Ndipo ufumuwu unatha pamene anthu a ku Asiliya anawatenga nawapititsa ku ukapolo, kuchokera pamenepa sitinvanso nkhani za ufumuwu. Ufumu wakumwera wa a Yuda unatha pakati pa zaka za m'ma 930BC mpaka 597 BC. Unakhala kwa zaka 333. Yuda anatengedwa ku ukapolo pamene anagwa m'manja mwa anthu akuBabulo.

2. Patatha zaka 70 AYuda ambiri anabwerera ku Yerusalemu kumene anakakhala pansi pa ulamuliro wa a Perisi.

3. Anthu a ku Gilisi ndi olowa m'malo awo analamula Israeli pakati pa zaka za 331 BC mpaka 164 BC. Pachiyambi pa ulamulirowu a Yuda analemera kwambiri. Izi zinasintha mu 198 BC pamene gulu lina la a Gilisi linatenga ulamuliro wa derali. Unali wa nkhaza kwa a Yuda kufika pa mfundo yowakakamiza kupembedza milungu yachikunja ndi kudya mkhumba.

4. ulamuliro wa nkhazawu unachititsa a Yuda kuukira ndipo anapambana zomwe zinachititsa kuti azilamulire okha kwaza zokwanira 100 kuyambira mu 163 mpaka 63 BC. Panthawiyi ndipamene magulu awiri osagwirizana anayambika muderali, kuYudeya ndi ku Israeli. Awa anali a Falisi ndi a Saduki amene kawirikawiri amalimbana ndi Yesu. Afalisi amakhazikika kwambiri pa chilamulo pamene a Saduki samavomereza za kuuka kwa akufa kotero samakhulupirira za gahena. Maguluwa amazuzulidwa kawirikawiri ndi Yesu. Magulu awiri amenewa anali m'dani kwa wina ndi mzache oti mu ulamuliro wa a Saduki a Falisi okwana 800 anapachikidwa pa mtanda.

5. kukula kwa chigiliki m'derali kunachititsa kuti Chipangano chakale chitanthauzilidwe mu chiyankhulo cha chi Giliki. Izi zinachitika ndi ophunzira 70 amene anagwira ntchitoyi payekhapayekha kuti zinthu zilongosoke. Ndipo ntchitoyi imatchedwa Sepitijuenti kutanthauza 70 (makumi asanu ndi awiri).

6. khalidwe lomenyana pakati pa Ayuda linachititsa aRoma kugonjetsa derali mosavuta. Awa anali mathero aIsraeli odzilamulira pa yekha kufikira pamene nkhondo yachiwiri pa dziko lonse inatha.

7. 6 BC ndinthawi imene imaganiziridwa kuti Yesu anabadwa, ndipo imfa yake inali mzaka za m'ma 30 AD. Sitidziwa bwino lomwe nthawi yomwe anakhala pano pa dziko la pansi.

8. pambuyo pa imfa ya Yesu, aYuda anaukira ufumu wa aRoma zomwe zinachitsa kuti anthu a nkhaninkhani afe pa chipolowechi. Ndipo pamapeto pake anagonjetsedwa mu 70 AD, ndipo kachisi ndi zina zambiri zinaonongeka panthawiyi. Ndipo aYuda otsala anakangamidzidwa kuchoka mu Israeli ndi kumwadzika padziko lonse lapansi. Ndipo analibe malo operekerapo msembe kwa zaka 2000.

Aroma analamulira mbali yayikuli ya dziko la pansi ndi madera ena a Africa ndi kum'mawa kwa Asiya (asia). Analimbikitsa Malamulo amene anachititsa bata muderali. Amalimbikitsa chiyankhulo cha chiGiliki chimene ndichiyankhulo chachikulu posanthula Baibulo. Chigiliki mwachitsanzo chili ndi mau ambiri omwe amatanthauza chikondi. Chili ndi mau a chikondi cha mwamuna ndi mkazi, komanso chikondi chapaubale komanso chikondi cha atate. Agilikinso anali ndi miseu yabwino yomwe imachititsa kuti chikhristu chifalikire muderali mwa nthawi yochepa. Mwanjira ina tinganene kuti, Mulungu anakonza nthawiyi kukhala yoyenera kuti Yesu akabadwiremo, ndikutinso uthenga ukarembedwe komanso chikhristu chikafalikire. Mwachitsanzo pamene mtumwi Paulo anafika ku Itale, anapedza akhrisitu akumudikira iye.

Chipangano Chatsopano chimanena za moyo wa Yesu Khristu pano padziko lapansi. Timaphunzira kwa iye kuti pali njira imodzi yopitira kumwamba, imene ndikuika chikhulupiriro chathu pa iye ndi kulola Mulungu Mzimu Woyela kulamulira miyoyo yathu.Tilape machimo athu ndikumutsata iye mukumvera konse. Zambiri muchipangano chatsopano ndi malangizo a m'mene ife tingakhalire ngati akhristu.

## ZENIZENI ZA UTHENGA WABWINO

Pali mabuku anayi muBaibulo omwe ndi a Uthenga wabwino; Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane. Mabukuwa amadziwika ndi maina a omwe adawalemba ndipo amanena za moyo wa Yesu mumagawo osiyanasiyana. Mateyu analemba buku lakeli kwa Ayuda kuwatsimikidzira kuti Yesu ndi Mesiya Mfumu ya muyaya. Marko analembera kwa akhristu akuRoma kuwadziwitsa za umunthu, ntchito ndi ziphunzitso za Yesu. Luka sanali muYuda ndipo iye analembera kwa anthu a mitundu. Cholinga chake kunali kumuonetsa Yesu ngati munthu weniweni komanso ngati Mpulumutsi weniweni. Yohane analembera uthenga wake kwa akhristu ongoyamba kumene komanso kwa anthu omwe si akhristu. Cholinga chake kunali kutsimikidza kuti Yesu Khrisitu ndithu ndi Mwana wa Mulungu ndipo onse okhulupirira iye akapedza moyo otsatha.

Mabuku atatu a uthenga wabwino amatchedwa senopitiki (synoptic). Mawuwa amachokera muchigiliki kutanthauza kuti 'limodzi' kapene 'zosasiyana'. Mabuku amenewa ndi monga ; Mateyu, Marko komanso Luka ndipo amakamba zankhani zofanana. Buku la Yohane liri ndi zina zomwe zimangopedzeka m'buku la Yohane lomweri basi. Kunanenedwa kuti ngati mabuku onse a muBaibulo akanasowa kupatula buku la Yohane, komanso Aroma chikhristu chikanakhalakobe.

Tiona magawo onse anayi a Uthenga wabwino kuphatikizapo Mateyu 5-7 chimene ndi chiphunzitso cha paphiri. Tiona zakufanana kwa Uthenga wabwino wachisenopitiki ndi Uthenga wabwino wa Yohane momwe umatsiyanirana ndi mabuku a chisenopitiki. Mwachitsanzo, Yohane sanena za fanizo lililonse ndiponso mwa zozizwitsa zisanu ndi ziwiri zomwe ziri m'buku la Yohane zisanu, sizikupedzeka mu mabuku enawo. Uthenga wabwino wa Yohane ukunena kwambiri za Mulungu zokhazokha ndipo umaona kwambiri za Yesu kuti ndi ndani ndiponso umafotokoza tanthauzo la chikhulupiriro mwa Iye.

## MATEYU

Mateyu amagwira ntchito yokhometsa misonkho yomwe inali yotsapatsa ulemu. Okhometsa misonkho amapeza ndalama munjira zopanda chilungamo. Pokhala ophunzira wa Yesu Khristu, zinaonetsera poyera kuti aliyense atha kukhala m'khristu ndikugwirisidwa ntchito ndi Mulungu muufumu wake.

1. Mateyu 1:1-17 amanena za mibado ya makolo a Yesu Khristu. Vesi 1 imatikumbutsa kuti ndiye mbeu ya Abrahamu komanso mfumu Davide. Ichi ndichinthu chabwino chifuwa chimakwaniritsa malonjezo oyambirira kuchokera kwa Mulungu.

A. kumbukirani Genesis 12:3 pamene Mulungu amamulonjeza Abrahamu kuti anthu onse adzadalitsidwa kuchokera mwa mbeu yake. Lonjezoli likukwaniritsidwa ndi Yesu. Kenako mu 1Mbiri 17:14 Mulungu anamulonjeza Davide kuti ufumu wake udzakhadzikitsidwa mpaka muyaya ndipo izi zikukwaniritsidwa ndi Mfumu Yesu Khristu. Masalmo 132:11 ndi Yeremiya 23:5 akukumbutsa anthu za lonjezo limeneri kuchokera kwa Mulungu.

B. Azimayi kwambiri satchulidwamo mu ndandanda wa makolo aYesuwa koma timawerenga za azimayi okwana khumi zimene zimatikumbutsa ife kuti Mulungu amachita zomwe sitimayembekedzera.

i. Mateyu mu vesi yachitatu akutikumbutsa za Tamala ndi nkhani yake yonvetsa chisoni yomwe imakhudza Yuda (Genesis 38: 1-30). Kumbukirani kuti Yesu ndi mbeu ya fuko la Ayuda.

ii. vesi 5 imanena za Rahabi yemwe anali oyendayenda.

iii. Rute akutchulidwa mu vesi 5 ngati kholo la Yesu. Kumbukirani kuti anali wakuMoabu. Limodzi ladziko lomwe linali paudani ndi aIsrael. Onani Deuteronomo 23:3-5 kuti muwerenge m'mene Mulungu anawaikira anthu am'dzikoli muthemberero.

iv. Vesi ya 6 ikulongosola za Betiseba mkazi wa Uriya, kuti ali mundandanda wa makolo a Yesu Khrisitu. Kumbukirani anali bwenzi la mfumu Davide mu chigololo ndi mukupha.

v. mzimayi otsiriza kutchulidwa mubuku la Mateyu ndi Mariya amake a Yesu. Yesu analonjezedwa kale mu Genesis 3:15. Kenako werengani Mateyu 1:18-23. Apa muona kuti kubadwa kwa Yesu Khristu kunalengezedwa iye asanabadwe. Mariya mayiwake ndiwapakati koma ndi namwali. Izi zikukwaniritsa ulosi wa Yesaya 7:14 muchipangano chakale.

Vi. Uchembere wa namwali otsadziwa mwamuna ndi wauzimu basi. Yesu ali ndi Mzimu Woyera ngati bambo ake pamodzi ndi Mariya, munthu weniweni ngati mayi wake. Kotero Yesu anali munthu weniweni komanso Mulungu weniweni. Sanachimwepo chifukwa anali Mulungu komanso anasangalasa mkwiyo wa Mulungu popedza anali munthu weniweni.

2. mutu 2 ndinkhani yomwe ikungopedzeka mubuku la Mateyu lokha ndipo ndi nkhani ya anzeru a kum'mawa. Anthu ambiri monga anzeru akum'mawawa anafunitsitsa kupembedza Yesu koma ena ngati mfumu Herodi anamuda iye nafuna kumupha. Mulungu anamutetedza Yesu poudza Yosefe kuti athawe ndikamwanako kupita ku Aigoputo kuti asaphedwe.

Zaka makumi atatu zikudutsa ndipo Yohane M'batizi akufika m'bwalo. Ntchito ya Yohane M'batizi ndikukwaniritsa chonenedwa muchipangano chakale ndi a neneri (onani Yesaya 40:1-5 ndi Malaki 4:5-6). Ntchito yake kunali kulengedza za kubwera kwa Mesiya. Werengani Mateyu 3:1-3. Kukonza njira yoti Mpulumutsi akafikiremo.

A. Ubatizo wa Yohane M'batizi siubatizo umene ife akhristu timachita. mukanabatizidwa ndi Yohane M'batizi kenako ndikukhala m'khristu pambuyo pa imfa ya Yesu mukanabatidzidwanso kawiri ngati m'khristu. Kumbukirani kuti cholinga cha Yohane M'batizi kunali kulengedza za kubwera kwa Yesu komanso kubwera kwa pangano latsopano. Ubatizo wa Yohane umakonzekeretsa anthu mukubwera kwa Khristu.

Kubatizidwa kwa Yesu kumaonetsa kutsasiyana kwake ndi aYuda ndipo izi zimalengedza kuti anabwera kudzakhala pamalo a wochimwa pansi pa chiweludzo cha Mulungu.

5. Pamutu wachinayi pali nkhani yomwe ikupedzeka m'mabuku onse a uthenga wabwino wa chisenoputiki. Mateyu 4:1-11 akunena za Yesu yemwe anatsogozedwa ndi Mzimu Woyera kupita ku chipululu kumene anakatsala kudya kwa masiku makumi anayi. Zitatha izi anayesedwa. Choyambirira anamuyetsa ndi chakudya popedza anali ndi njala ndipo amafuna chakudya kuti adye. Yesu anagonjetsa mayetsero onse ndipo sanagwe mutchimo ndi mayeserowa. Kuyesedwa si tchimo. Limakhala tchimo pamene tigwa m'mayetserowo ndikuchita uchimo. Yesu anati ayi kumayetsero onse a Satana ndipo sanachimwire Mulungu Atate.

6. Yesu anayamba utumiki wake Yohane M'batizi ali kundende. Mateyu 4:17 amati uthenga wake unali wakuitanira anthu kuti alape zomwe zimafanana ndi ulaliki waYohane M'batizi. Anayambanso kusankha ophunzira ake. Vesi 18 ikuonetsa ophunzirawa monga Simoni Petro ndi Andreya amene anali asozi amsomba. Vesi 19 ikunena za cholinga chimene anawaitanira iwo. Anawaitana iwo kuti akhale asozi a anthu. Zomwe zikutanthaudza kuti anaitanidwa ndi cholinga choti akathandize kuitanira anthu kuufumu wa Mulungu.

7. Mutu 5-7 ukuyankhula za chiphunzitso chapaphiri. Timawerenga kuti Yesu anapita kuphiri ndi anthu ambiri ndipo anakhala naphunzitsa iwo chiphunzitso chopanda banga. Ichi ndi chiphunzitso chofunikira kwambiri ndipo chiyenera kuphunzitsidwa m'matchalitchi athu onse.

A. Werengani mutu 5:2-12. Awa amatchedwa madalitso a anthu odala. Werengani ndikukambirana za iwo.

i. Vesi 3 imati osauka muuzimu ali odala. Izi zitanthauza kuti ndidalitso kunvetsetsa za umphawi wako muuzimu pamaso pa Mulungu kotero kuti utha kudalitsidwa ndi Mulungu.

ii. muvesi 4 timawerenga kuti odala ali achisoni chifukwa adzasangalatsidwa. Chisoni chimakhala pamwamba. Timatonthodzedwa ndi uthenga wabwino umene umanena za kukhululukidwa kwa machimo.

iii. vesi 5 ikuti odala ali ofatsa. Mau ofanana ndi kufatsa ndi kudzipatsa ulemu. Izi sizitanthauza kukhala wa mantha. Kumbukirani Numeri 12:3 pamene timanva kuti Mose anali ofatsa kupotsa onse padziko lapansi. Vesiyi imachokera ku Masalmo 37:11ndipo imatanthauza kulandira chilichonse chomwe Mulungu apereka kwa ife ndikukhutitsidwa nacho. Sitiyenera kuyambitsa chisokonezo pamene tifuna zochuluka zomwe sitinapatsidwe.

iv. odala ali akunva njala ndi luzu la chilungamo. Anthuwa ndi odala chifukwa akhumba kuyenda njira zokondweretsa Mulungu. Izi ndizotheka pamene uli pa ubale wabwino ndi Yesu. Tikhale ndi khumbo kuti tikhale achilungamo monga Yesu Khristu amene anali komanso ali wachilungamo.

v. vesi 7 ikuti odala akuchitira chifundo. Chifukwa chifundo ndichomwe timalandira pamene tapulumutsidwa. Ili ndi khalidwe la mkati ndipo ife timadala pamene tichita chifundo chotere kwa anzathu. Onani Mateyu 18:21-35 pamene tikunva za fanizo la kuchitira ena chifundo. Tikuona mfundo yakuti timayembekedzera chifundo kuchokera kwa Mulungu komanso kwa anthu koteronso ife tichitire ena chifundo. Onani Mateyu 6:12 amene achitira umboni pa zomwe tinenazi. Kumbukirani kuti chifundo chikhululuko komanso chiyanjano zili pa ntima wa chikhristu.

vi. odala ali oyera mtima. Miyambo 24:3-4 akuchitira umboni pa nkhaniyi. Ndife odala pamene mitima yathu ikhala yoyera chifukwa tidzaona Mulungu.

vii. vesi 9 ikuti, odala ndife pamene tichita mtendere. Izi zingatere pamene tigawana ndi anzathu uthenga wabwino omwe umapanga munthu kukhala pa mtendere ndi Mulungu. Zimatanthauzanso kwa ife kuti ngati anthu odala tiyenera kuthandidzira kuyanjanitsa anthu amene ali pamakangano maka iwo amene ali akhristu.

viii. vesi 10 ikuonetsa chinthu chimene ndichovuta ndi akhristu. Koma ngakhale ndichovuta tiyenerabe kudziwa kuti tili odala pamene tidzudzidwa chifukwa cha chilungamo. Dziwani kuti Yesu salonjedza nthanzi kapena chuma. Vesi 11 ndi 12 ikuti tidzalandira mphoto chifukwa cha ubale wathu ndi Yesu ndipo ichi chidzabweretsa nsauko pakati pathu. Ndife odala ndipo chifukwa cha chilungamo ndi Yesu titchulidwanso a chilungamo. Titha kutsautsidwa chifukwa cha ubale wathu ndi Yesu, koma vesi 7 ikuti, izi ndi zakanthawi kochepa ndipo tidzalandira mphoto yamuyaya kumwamba pamapeta pa zonse. Pakadalipano akhristu akutsautsidwa pano padziko la pansi.

B. Vesi 13-16 ndimavesi otchuka amene amanena za kuunika ndi mchere. Ndife mchere pamene tithandiza dziko kuti lisagwe mum'dima wa ndiwe yani. Komanso ndife kuunika pamene tibukitsa kuunika kwa uthenga wabwina kwa anthu onse. Ndipo umboni wathu ndichinthu chofunikira kopotsa.

i.Tingasukuluke bwanji? Tingasukuluke pamene tilephera kuonetsa kuwala kwa Yesu Khristu kapena mwanjira ina pamene tilephera kuchita zomwe Yesu akufuna kuti tichite.

ii.Ndife mchere ndikuunika pamene tinvera ndikutumikira Mulungu mokhulupirika. Timakakhala kuunika pamene tigawana uthenga wabwino ndi anzathu.

C. Mateyu 5:20 akunena za lamulo la chipulimutso. "pakuti ndinena kwa inu kuti ngati chilungamo chanu sichipotsa cha alembi ndi afalitsi simukhodza kulowa muufumu wa Mulungu. Fotokozani m'mene timakwaniritsira izi kuchipulumutso chathu. Kodi tingakwaniritse izi podalira mphavu zathu?

D. Mavesi osatira pamenepa muchaputala chimenechi maka vesi 21-23 timaphunziramo zakukhala mumtendere ndi anthu onse. Timaphunzira kuchokera mu vesi 21-22 kuti mkwiyo wa muntima umachitisa tchimo lamuntima. Timachita tchimo la kupha pamene tikhumba mzathu atafa. Tikuona kuti mkwiyowu umakhala waukulu kuti sizitheka kupembedza Mulungu pamene sitikhala muntendere ndi anzathu. Dziwani kuti palibe ndim'modzi yemwe anakwiyitsa moyo wanu kopitirira mwezo kupotsa m'mene tchimo lanu limakwiyitsira Mulungu. Ngati tifuna Mulungu kuti atiyanjanitse ife ndi Iye mwini komanso kutikhululukira machimo athu tiyenera ife tiyanjane komanso kukhululukirana wina ndi nzache.

8. Mutu wa chisanu umanena za mulingo wa chilungamo omwe ife tiyenera kukhalamo. Njira ina yokambira izi ndi m'mene akhristu akhalira omwe uli umboni wao. Tiyenera kumuonetsa Yesu kudziko lapansi.

A. muchaputara cha 6:9-13 Mateyu akutiudza kuti tiyenera kuchita zabwino mwachinsisi monga ngati kuchita zachifundo komanso kupemphera. Akuti kupemphera ndi kuchita zachifundo kusalekeke, koma kuchitike mwachinsinsi otsati anthu adziwe ndikutitcha ife abwino. Ife siandale amene amafunafuna mavoti koma ife timafuna kusangalatsa Mulungu kotero sitiyenera kuulutsa zonse zomwe tikuchita kwa ena. Mulungu amadziwa zonse zomwe tikuchita. Kumbukirani kuti ulemerero upite kwa Mulungu pa zonse tidzichita.

B. Akutiudzanso m’mene ife tingapempherere moyenera. Sitiyenera kubweredza bweredza pamene tipemphera. Pamutu wa 6:9-13 Yesu akupereka chitsanzo chabwino cha pemphero. Ngakhale ndikwabwino kupemphera monga mavesiwa anenera, komabe titha kuyenjedzeramo mau ena popemphera.

C. Vesi ya 16-18 ikunena dzakutsala kudya. Dziwani kuti vesi 16 ikuti pamene mutsala otsati ngati mutsala. Zikutanthaudza kuti tiyenera kutsala kudya. Tikumbutsanenso kuti tiyenera kuchita izi mwachinsisi ngati ichi sichili champingo onse.

D. Kubweredza; mutu 6 ukutiphunzitsa kuchita zinthu zabwino koma mwachinsisi ngati izi ndizotheka kutero. Sitiyenera kuchita izi pofuna kukudza munthu. Osati tichite izi kuti anthu aone kuti ndife abwino. Tichite izi ponvera ndi potsangalatsa Mulungu. Kupemphera kwathu ngakhale kupereka kwathu zichitike mwamseri pakati pa ife ndi Mulungu wathu.

i.ngakhale sitiudza anzathu kuti ndife a khristu, zintchito zathu zichitire umboni kuti ife ndife akhristu. Zimakhala bwino kuti anthu akaziwe kuti ife ndi akhristu ndizintchito zathu.

E. Vesi ya 14 ikutiudza kuti khalidwe lathu pa chikhululuko likhalebe. Tikhululukire iwo amene afuna chikhululukiro. Ganidzirani m’mene Mulungu wachitira kwa ife pakutikhululukira.

F. vesi 19-24 ikukamba za ndalama ndi chuma. Werengani ndikuthira ndemanga za m’mene tingapewere kuyenda ndi ndalama, ndikuyetsetsa kuyenda ndi ntchito zabwino.

G. 25-34 pali malangizo okhudzana ndikudera nkhawa…… ndikwabwino kukhulupirira Mulungu wamphavuyonse. Onani Aroma 8:28.

9. Mutu wa 9 ukuphunzitsa zakuwerudza ena, zokhuzana ndikupempha Mulungu, komanso za mtengo ndizipaso zake. Tinena za kuweruza ena pa Luka mutu wa 6.

A. vesi ya 12 ili ndiphunziro labwino lomwe tikulitcha “lamulo lopambana”. Mwanjira ina tinganene kuti tipangire anzathu zomwe ife timafuna kuti ena atichitire. Tichitire anzathu zabwino. Mumasangalala mukamagawira ena zomwe mulinazo?

B. 21-23 ndimavesi amene amapereka chiopsezo muBaibulo monse. Apa Yesu akunena ndi akhristu makamaka anthu ngati ine amene timaphunzitsa Baibulo. Tionetsetse kuti ndithu tili mwa Yesu. Tikumbukire kuti Mulungu amagwiritsa ntchito ngakhale otsatembenuka mitima kukwaniritsa zolinga zake.  Zoti ndinu m’busa kapena m’mkulu wampingo sizitanthaudza kuti ndiinu opulumutsidwa.

C. 24-27 ikuti, mangani Nyumba yanu pathanthwe. Kodi mwalawu ndiyani amene sogolo lathu liyenera kumangidwapo?

D. vesi 29 Yesu akuphunzitsa ndiulamuliro umene anakhala nawo chifukwa ndi Mulungu.

10. Mutu 8 ukunena za zozizwitsa zomwe Yesu adachita. Mutu 7 ukutsekedwa ukuonetsa Yesu ngati kuti ali ndi ulamuliro onse potsimikidziridwa ndizozizwitsa zomwe akuchita. Chimodzi cha zolinga za zozizwitsa ndikutsimikidzira kuti Yesu ndi Mulungu.

A. 18-22 timaphunziramo zimene ambiri amanyalanyaza komanso otsalabadira. Kukhala m’khristu sichiyembekezo chamoyo wathanzi, chuma kapena ulemerero ayi; koma ndichipsinjo.

11. Mutu 9: 35-38 umakamba za anthu ochuluka kuti afikiridwe ndi uthenga wabwino, komanso kuchepa kwa iwo otumikira uthenga umenewu. Tikulimbikitsidwa kupempherera chinthuchi. Pamene mupepherera anthu kukhala mamitchonale padziko lapansi pemphani Mulungu ngati afuna inunso kuti mupite nawo. Muli okonzeka kutumikira Iye?

12. Mutu 10:5-15 tikuona za ulendo oyamba opita kuutumiki. Atumwiwa analipo 12 kukatumikira Nyumba za aYuda okhaokha. Siinali nthawi yofikira amitundu ndiuthenga wabwinowu.

A. vesi 1 ndi 8 zimatanthauziridwa molakwika. Ndiophunzira okha amene adapatsidwa mphamvu zochiritsa odwala. Akhristu ena lero amaganiza kuti alinso ndimphamvu yonga yomweyi, koma izi sizoona ayi. Mphamvu zomwe tilinazo ndizongopempha Ambuye kuti achilitse odwalayo. Vesi 8 ikuti asalipiritse. Tisamalipiritse pamene tipempherera kapena kutumikira akhristu anzathu.

B. vesi 15-23 tikuona Yesu akuphunzitsa kuti uthenga woyang'ana za thanzi, chuma ndi ulemerero sioyenera. Onaninso m'mene akulonjedzera nsautso kwa ophunzira ake ankansatabe iye. Ilinso ndi phunziro kwa ife tonse.

i.konzekani kukumana ndi m'sauko komanso kuimabe ndikukhalabe muchikhulupiriro ndikusaleka kutumikira iye.

ii.vesi 19-20 ikutikumbutsa kuti Mulungu Mzimu Woyera akhalebe nthandidzi wathu. Onaninso Machitidwe a Atumwi1:8 pamene Yesu akulonjeza Mzimu Oyera kudzatitsogolera ife. Adzakupatsani mphamvu yakuchita chilichonse chomwe Mulungu afuna kuti inu muchite.

C. Vesi 28 pali malangizo ofunikira kwambiri. Mavuto athu m'moyo uno siodandaulitsa kwambiri. Posachedwapa tilekana ndimoyo wamavutowu. Ndipo akhristu amayang'ana moyo ulinkudzawo womwe udzakhale kwa muyaya. Moyo uno ndi wakanthawi kochepa.

D. Vesi 32-33 tikuphunzira kulankhula mwa mphamvu zokhuzana ndi Yesu kwa ena ndipo izi zidzapangitsa anthu kuzindikira kuti ife ndi ophunzira ake.

13. Mutu 11:1-15 ngakhale Yohane M'batizi amene anali mundende samadziwa bwinobwino za Yesu Khristu. Pomutsimikidzira Yohane za iye, Yesu anamuonetsa zonse zozizwitsa zimene adazichita zomwe zimasimikidzira kuti iye ndiye olonjedzedwayo. Dziwani vesi 11 imaphunzitsa kuti wamng'ona ku ufumu wa kumwamba ndi ali ndiudindo waukulu kwambiri kupotsa munthu waulemu padzikolonse lapansi.

14. Mutu 12:1-21 kulimbana ndi Yesu kukupitirirabe pamene Afarisi akunyasidwa chifukwa Yesu sasatira Malamulo amene iwo adawayenjedzera kuBaibulo. Nkhani ndi yakasungidwe ka sabata. Vesi 1-18 ikukamba za kukolola ndikudya patsiku lasabata. Kenako vesi 9-13 Yesu akuchiritsa patsiku la sabata. Vesi 14 izi zikupangitsa Afarisi kukonza za imfa ya Yesu.

A. Mateyu 12:3-8 mfundo zitatu zokhuzana ndi sabata

i. munthu ndiopambana kupotsa kumvera Malamulo. Luka 14:15

ii. sabata inapangidwa chifukwa cha munthu; ndimphatso yochokera kwa Mulungu. Marko 2:27

iii. Marko 2:8 Yesu anaphunzitsanso kuti iye ndiye Mbuye wa Sabata-Yesu analengedza kuti ndiye wochokera kwa Mulungu. Mwanjira ina Yesu ndi bwana wasabata. Ndiiye amene amapanga Malamulo.

James Boice pankhani yasabata akuti “ndikukhala m’makhalidwe amene angalemekedze Ambuye Yesu ndikukwedza iye. Ndiokhulupirira okha amene amasangalala nditsiku la sabata. Sangalalani pakupembedza, pachiyanjano komanso ndi banja lanu. Pamafunika kupumula pazonse zomwe timachita tsiku nditsiku.

B.Afarisi adayenjedzera zambiri ku Baibulo zomwe zinapangitsa moyo kukhala ovuta zedi. Pansipa, pali zina mwa zomwe adayenjedzera ku lamulo la sabata monga anenera James Boice. Awa anali Malamulo amwe amaonetsa kuti amatsatira zolembedwa za m’malamulo a Mose, koma zoona zake zinali zakuti lidali khalidwe lokana Malamulo a Mulungu. Mwanjira ina, omaoneka onvera lamulo m’maonekedwe, pamene mkati mwao amatsutsana ndi lamulo. Kotero uku kumangokhala kutonza ndi chibwana.

*“ Afalisi adayenjedzera zoletsa za munthu mu Malamulo a Mulungu, kuchotsa zoyenera kutsunga patsiku la sabata ndikuika zina zachilendo komanso zovuta. Mwachitsanzo;*

*1.Lamulo limati munthu atsayende patsiku la sabata(Eksodo 16:29). Ndizonveka ndithu! Koma izi zimatanthauzanji? Afarisi anafunsa. Ngati yankho amati munthu aziyenda mamita okwanira 300 basi patsiku lasabata. Ngati munthu apitira marire amenewa ndiye kuti wachita tchimo. Ngati mudzi watchingidwa ndi chingwe, ndiye kuti mudziwo ndiwo malo omasuka kuti munthu akayendemo. Koma ngati muthu atuluka kunja kwa mudziwo asayende mamita okwanira 300 kupambana chingwecho.*

*2. lamulo limaletsa munthu kunyamula katundu patsiku la sabata (Yeremiya17:21-27). Koma katundu ndichiyani? Kodi chovala ndikatundunso? Afarisi amati ngati chovalacho chavalidwa sichikhala katundu, koma ngati changonyamulidwa chimayesedwa kuti ndi katundu. Ndiye ngati ukufuna kusamutsa jekete kuipititsa kuchipinda china patsiku lasabata umangoyenera kuivala kuti upite nayo chipinda chinacho.*

*3. lamulo limaletsa kugwira ntchito pa sabata. Izi zimayenda motere. Munthu akuyenda panseu, ndipo waganidza zolavula malovu, kodi imeneyinso ndi tchito? Yankho linali lakuti zimatengera chomwe malovuwo achite akalavulidwa. Ngati malovuwo agwera panthaka nayendapo pang’ono ndiye kuti ntchito yagwirika pamenepo. Ngati malovuwo agwera pamwala ndiye kuti sipadachitike ntchito. Mwanjira iyi, ngati mfarisi wokhwima zimaoneka ngati walavula moyenera patsiku la* sabata”.

15. Mateyu 23:28 tikuona za maganizo amene tingawaike kuchokera muchiphunzitso cha Baibulo zokhudzana ndi sabata. Tiyenera kudya komanso kuchita ntchito za chifundo. Yesu akuti, zimatengera khalidwe la mtima wa munthu ndipo osati maonekedwe awo akuthupi. Koma ndi Afarisi chinangokhala chabe chionetsero. Yesu anaonetsa kulephera kwa chipembedzo chao ndipo adakwiya ndizimenezi.

A. ndichifukwa ninji timatenga sabata kukhala laMulungu otsati loweruka?

i. Yesu adauka kwaakufa tsiku laMulungu.

ii. Machitidwe Atumwi 20:7 imaonetsa kuti akhristu oyamba amakumana laMulungu.

iii. mpingo woyamba unakumana ndi zokhoma ndi otembenuka kuchokera

> kwa Ayuda poyetsa kupanga chikristu kukhala mbali imodzi ya chipembedzo cha Ayuda.

Otembenuka achiyudawa amaganidza kuti chikhristu chimafunikira kumasunga Malamulo aChipangano Chakale. Kunali kofunikira aliyense kudziwa kuti chikhristu chinali chotsiyana;

Chipangano chakale chapita ndipo chatsala Chatsopano. Kupembedza tsiku lotsiyana kumathandidza motere. Mpingo woyamba anasankha matsiku otsiyanakupotsa aYuda amene amasala kudya sabata iliyonse kutsimikidza kuti chikhristu chinali chotsiyana ndichipembedzo cha aYuda.

16. Mateyu 12:22-32 akunena za tchimo lotsakhululukidwa. Vesi 24 ndilo khama la afalisi kudetsa Mbiri ya Yesu. Amati amachita zozizwitsa kudzera mumphamvu ya Satana. Vesi 31 ikunena za tchimo lotsakhululukidwa lomwe ndikunyoza Mzimu Woyera. Kodi tchimo limeli ndichiyani? Yankho- Ndi Mzimu Woyera amene amatiunikira kuti tivomeredze Uthenga Wabwino. Tchimo losakhululukidwa ndiko kukana Mzimu Woyera ndi Mulungu ndikuumitsa mitima yao pokana Yesu. Munthu amene amachita tchimo ili salabadira za ichi, choncho ngati inu mwakhudzika dziwani kuti simuli opalamula tchimoli.

17. Mutu 13 ukunena za mafanizo. Fanizo ndi nkhani yomwe ili ndi tanthauzo. Tingavetsese bwino fanizo pamene tili paubale wabwino ndi Yesu. Kuti tinvetsese fanizo tiyenera tiyang'ane mfundo yomwe yamangirira nkhaniyo. Werengani 13:1-9 Fanizo la ofetsa. Onani vesi 18-23 kuti muone kufotokodzera kwa Yesu Khristu. Mbeu ikukambidwa ndi Uthenga Wabwino ndipo nthaka ndi mtima wamunthu. Mitundu itatu yamitima yafotokodzeredwa yomwe imanva mau kumapeto kwake kumukana Yesu. Ndipo ntima wotsilidza umanva mau ndikutembenukira ku chikhristu. Tikuphunzira kuti

A. sionse amanva mau kuti ndiakhristu. Uyenera kukhala ndi mzimu wotseguka kuti ukhale mkhristu weniweni.

B. timaoneka kuti ndife akhristu pamene tionetsa zipaso zomwe zitanthaudza kuti timachita ntchito zabwino ndipo tiyamba kukhala m'makhalidwe amene Yesu amafuna kuti tikhalemo.

C. tiyeni tione fanizo lina pavesi 44-45. Mfundo yaikulu mufanidzoli ndiyakuti athuwa anapedza ufumu wakumwamba kukhala opambana kotero kuti adalola kupereka chilichonse adalinacho ndikupedza moyo osatha.

D. Fanizo lina lokhudzana ndi nkhoka likupedzeka pa mutu wa 13:47-50. Iyi ndinthawi yachiwiri pamene Yesu m'mutu wa 13 akuphunzitsa phunziro lofanana. Onani fanizo la kutentha nansongole muvesi 24-30. Yesu akuphunzitsa m'mene akhristu ndi ndiachikunja adzalekanitsidwe patsiku lotsilidza. Omwe siakhristuwa adzaponyedwa malo amsautso. Ndipo sipadzakhala chiyembekedzo chakuchoka kumalo oipawo. kugahena ndikosabwerera komwe kudzapange okhalakowo kupanda chiyembekedzo. Onani Mateyu 25:46 ndi Marko 9:43 komanso Luka 16:26.

i. Tinvetsetse kuti kumwamba ngakhale kugehena ndi kunsabwera. Anthu ambiri komanso azipembedzo zonyenga amati otsaopa gahena chifukwa sizoona kuti iliko ndipo amati ngati ilikodi sikoyipa kumaloko komanso sikwamuyaya. Osakhulupirira amati asanabadwe samadziwa chilichonse, akadzamwaliranso sadzadziwanso chilichonse. Koma angoziputsitsa okha, panthawi yomwe adzamwalire ndipamene adzawona kuti Baibulo limanena zowona; kuti gahena ndioopsa ndiponso munthu sangachokeko pamene wangofikako, koma nthawi idzakhala itatha.

18. mutu 14:13-21 akunane za m'mene Yesu anadyetsera anthu okwana 5000. Nkhaniyi imaonetsa chifundo cha Yesu Khristu kwa anthu anjala ndinso m'mene angakwaniritsire zotsowa zathu.

19. Mutu 16:21-23 Yesu akuwakonzekeretsa ophunzira ake pa imfa imene ikubwera pa sogolo pake. Ziwani yankho la Petro ndi chidzudzulo cha Yesu kwa Petroyi. Imfa ya Yesu

pamtanda inali pulani ya Mulungu kugonjetsa Satana komanso kutiombola ife. Kutsusana ndi ichi ndikutsusana ndi Mulungu. Kumbukirani kuti Yesu ndiye amene alamulira zonse.

20. Mutu 16:24-25 tikuonanso zakuti tisautsidwa ndikubuma kwakukulu chifukwa chakutsata Yesu. Ngati fanizo lomwe taliona pa mutu wa 13:44-46 akuti tikonzeke kupereka chilichonse nsembe chifukwa cha ufumu wakumwamba. *Werengani khani ili m'musiyi yomwe ikunena za zomwe zinachitika ku America potsachedwa. Ndinkhani ya msikana wa zaka 17 yemwe anali msilamu masiku am'mbuyomo ndipo anaphedwa atangolowa chikhristu. Koyamba makolo ake anayetsera kumubwedzeretsa muchisilamu, kenako anayamba kumudzudza, ndipo chifukwa cha nkhadzazi anathawa napita kutali. Ndipo aaphedwa ndi m'madzi mwa athu a m'banja lomwe amakhalanao. Mtsikanayu anadziwa kuti kutsata Yesu umayenera kupereka dipo, ndipo ndimtima wonse adapereka dipo limeneli chifukwa cha Yesu.*

21. Mutu 17:1-8 tikuona za ku kusandulika kwa Yesu. Marko ndi Luka akunenanso zimenezi, ndikuchitiridwa umboni pa 2 Petro 1:16-18. Kusandulikaku kunali vumbulutso la umulungu wa Yesu Khristu. *Kusinthika kumeneku kunali kwa kanthawi kochepa komanso kosakhalitsa kuchokera kumene kunabitsika ulemerero wake pano padziko lapansi ndichionetsero cha ulemerero umene udzavumbulutsidwe bwino lomwe nthawi yakubwera kwake kachiwiri. Mulungu mukukusandilikamo amaonetsa kuti kodi Yesu ndi ndani; ndi Mulungu.*

22. Mutu 19: 3-9 tikuphunzirapo za banja komanso za chirekaniro. Tikudziwa kuchokera mu buku la Genesis 2:24 kuti pamaso pa Mulungu timakha munthu m'modzi pamene talowa m'banja. Ndipo tikuyenera kukhala chomwechi mpaka kale.Yesu anagwiritsa vesi lomweli ponetsa kutsakondwa kwake pankhani ya chilekaniro. Adati Moses anavomeredza chilekaniro chifukwa cha kuumitsa mitima yao. Apa Yesu akunena kuti ngati m'modzi wachita chigololo banja litha kutha ndipo winayo ali mfulu kukwatiranso. Komabe banja litha kupitirira. 1 Akorinto 7:15 akulolansa banja kutha ngati wosakhulupirira wasiya wokhulupirira. Ichi ndichapaderadera. Koma zifukwa zina kupatula ziwirizi sizovomeredzeka, ngakhale ena amati pamene wina achita nkhadza kwa nzakeyo banja litha kutha. Kutha kwa banja kumadzudzitsa anthu atsalakwa makamaka ana. Anthu amene akhudzika ndi kulekana kutha kwa banja tikuyenera kuwatsamalira kopotsa. Kutha kwa banja chimakhala chinthu chopweteka kwambiri. Ngati mpingo tifikire mwachikondi iwo amene akhudzika ndikutha kwabanja.

Tiyeni tione Mabuku ena a Uthenga wabwino ndiziphunzitso zake. Sitiphunzitsa zabuku la Marko chifukwa lili ndi uthenga wopambana choncho sitingauphunzitse mwachidule koma ufunika kuuphunzira modekha.

## ZIPHUNZITSO ZA BUKU LA LUKA

Luka akupereka zambiri za moyo wa Yesu Khristu akadali mwana. Luka sanali muYuda koma adali dotolo. Ndiyemweyenso amene adalemba buku la Machitidwe a Atumwi. Akutionetsa chithunzi chenicheni cha kumwamba ndi kugahena. Akuphunzitsa zambiri zokhudzana ndi pemphero. Tilibe nthawi yambiri younikira buku lonse koma tingoona ziphunzitso zina zomwe sidzipedzeka mu mabuku enawa.

1.Luka 1:26-56 akunena za Maliya, anali munthu wopatulika ndithu koma sadali Mulungu momga matchalichi ena amanenera. Adalinso ochimwa ngati ife tomwe, ndipo iyenso ankafuna chipulumutso. Osapemphera kwa iye chifukwa alibe mphavu zapaderadera.

2. Luka 2:8-20 angelo akudziwitsa za kubadwa kwa Yesu kwa anthu osatengedwa ngati kanthu mu dera – abusa a ng'ombe. Yesu anabwera kudzatumikira kwa anthu ngakhale otsayetsedwa ngati kanthu padziko lapansi. Makamaka osauka.

3. luka 4:16-30 Yesu ayamba utumiki wake atatha kuyetsedwa ndi Satana muchipululu. Adayamba ndikuphunzitsa musinagogi kudera la kwao ku Nazareti. Tikuona kufunikira kwa mapemphero a pagulu chifukwa Yesu adateronso kwao.

A. Vesi 16-21 tikupedza Yesu akuphunzitsa powerenga Malemba kwa anthuwo. Adagwiritsa lemba la Yesaya limene ndi ulosi okhudzana ndi Mesiya. Akutero kuti iye, Yesu ndiye olonjezedwayo. Mwanjira ina Yesu akuti iye ndiye Mesiya.

b. Iye (vesi 25-26) akunena za Eliya momwe adapitira ku malo achilendo ku Zerefati kukatumikira mkazi wa masiye.

C. Yesu (vesi 27) akunena za mulendo Namani ndimachiliso omwe adawalandira. Uthenga uwu kwa Ayuda udali kufuna kuonetsa kuti Mulungu si wa Ayuda okha. Mulungu ndi wa anthu onse a padziko la pansi.

D. Vesi 28-29 akunena kuti zitsanzo zitatu zili pamwambapa zinayipira Ayuda kwambiri. Choyamba adakwiya chifukwa adazitchula yekha kuti ndi Mulungu. Kenako adanyasidwa naye kopotsa chifukwa adati, Mulungu ndi wa anthu onse a padziko la pansi osati Ayuda okha. Ndizovuta kunvetsa kuti ndichifukwa ninji Ayuda amachita Nsanje ndichimenechi. Koma Mulungu ndi kumwamba ndi zazikulu kukwanirawina aliyense.

E. Ayuda adafuna kupha Yesu. Koma timawerenga vesi 30 kuti Yesu adachoka kwa iwo. Siidali nthawi yoyenera kuti iye afe. Zikuonetsa kuti ndiye olamula sono otsatinso Ayuda. Tikumbukire kuti Yesu adafa pantanda mozipereka chifukwa cha chikondi chake cha kwa ife. Palibe adamukakamidza pansi pano kuti akafe pamtanda

4. Luka 5 akunena za m'mene Yesu adaitanira ophunzira ake. Tikuona kuti adasankha anthu wamba monga asozi.

A. Vesi 27-32 ikunena kuti Yesu adayitana ngakhale okhometsa misonkho. Levi okhometsa misonkho (dzina lina la Mateyu), adadyetsa Yesu ndi okhometsa misonkho anzake m'nyumba yake. Apa timawerenga za zomwe afarisi adayankhula ataona izi. Adazuzula Yesu kuti akuyanjana ndi ochimwa.

i. Vesi 31-32 ikutiphunzitsa za ulaliki. Nthawi yathu yambiri idzithera kulalika uthenga wabwino kwa ochimwa. Akhritu amakonda kutha nthawi yao ndi akhristu anzao. Chikhale chikhumbokhumbo chathu poika moyo wathu kwa anthu ochimwa kuti nawo apedze chipulumutso monga momwe Yesu amachitira.

B. Vesi 33-39 ikutiudza za zinthu zingapo

i. ngakhala sitinalamulilidwe kuti tidzitsala kudya,Yesu akunena pa vesi 35 kuti adzatsala kudya pamene iye adzakwere kumwamba. Koma pamene ali ndiophunzira ake sayenera kutsala. Komabe kusala kudya sichinthu chochitika pa mtendere koma pamene pali mavuto ndipo potsalira kudya. Ophunzira ake ndiotsangalala pamene Yesu ali nawo pamodzi.

ii. chifukwa chimene akhristu amasalira kudya ndi chotsiyana ndi zifukwa za muchipangano cha kale. Yesu angwiritsa chitsanzo cha matumba a vinyo atsopano pofuna kuonetsa chisangalalo mu pangano la tsopano; njira ya tsopano yotsalira kudya komanso yotumikira Yesu. Pangano lakale lodzala ndi malamulo silinali labwino ayi, pamene pangano latsopano ndi Yesu ndilabwino kwambiri. Sitifuna kuphatikidza pangano latsopano la chitsomo ndipangano lakale la lamulo ndi ntchito.

iii. Vesi 39 ikunena kuti afalisi ndi ophunzira awo akukana kuvomeredza pangano latsopano lachisomo lomwe lili ndi lonjedzo lamoyo wosatha. Adafunitsitsa kutsunga pangano lakale limene silikhodza kupulumutsa aliyense. Anthu kawiri kawiri amakonda kutsata njira zakale zopangira zinthu ngakhale zatsopano komanso zophweka akudiwona. Tikuyenera nthawi zonse kutengera njira zatsopano zimene Baibulo likutiphunzitsa.

5. Luka 6:37-38 ndi 41-42 komanso Mateyu 7:1 tikuonamo za kuweruza zomwe anthu sazinvetsetsa. Iyinso ndi mbali ya chiphunzitso cha paphiri. Pali nthawi yomwe tiyenera kuwerudza ena. Mwachitsanzo titha kugwiritsa ntchito Baibulo lathu kuona ngati olalika akulalikira zinthu zoona. Tikuyenera kuwerudza m'moyo wathu watsiku ndi tsiku.

A. tikuudzidwa kuti otsati tikhale anthu okonda kupedzera anzathu zifukwa nthawi zonse, makamaka atsogoleri ampingo wathu. Sitiyenera kukhala oyambitsa vuto pamalo; sitiyenera kukhala amiseche. Onani vesi 41-42 kuti munvetsetse nkhaniyi. Mfundo ndiyakuti tonse tikuyenera chiwerudzo chifukwa ndife ochimwa muzinthu zambiri. Tionetsetse kuti sitikhuzika ndicholakwika kuti tikwanitse kuwerudza ena moyenera. Tisaweruzenso mwachangu ndimolakwika ayi. Tiwerudze ngati ifenso tifuna kuweruzidwa.

6. Luka 6:39-40 ndifanizo limene likupereka chitsanzo cha vuto la mumpingo lomwe tikuthandidzira kulithetsa. Ndichifukwa chimene m'firika ayenera kuphunzitsa m'firika nzake zachimene Baibulo likuphunzitsa. Tiyenera kukhala ndi akulu ampingo ophunzila bwino zachimene Baibulo likuphunzitsa kuti aphunzitse anthu awo ndikuthandidza mpingo kuphunzira Zoona zoona zokhuzana ndi Mulungu.

A. Vuto loyamba lomwe tikuliona mu vesi 39 ndilakuti, tili ndi akulu a mpingo amene sadaphunzitsidwe Baibulo omwe amaphunzitsa mpingo zinthu dzokhudzana ndi Mulungu. Ichi ndichitsanzo chawakhungu kutsogolera wakhungu mzake.

B. Vuto lachiwiri tikuliona pa vesi 40. Cholinga cha mpingo pophunzitsa ndi kulalikira ndiko inde kulemekedza Mulungu zimene munthu amachita pamene waphunzira zambiri zokhudzana ndi Mulunguyo. Ngati m'busa ndiophunzira bwino Baibulo, atha kuphunzitsa bwino mpingo wake ndikuthandidza anthu kupita chitsogolo. Ngati mkulu wa mpingo wapita chitsogolo ndi phunziro la Baibulo; angathandidzenso kupititsa patsogolo anthu ake pakuwagaira zomwe amaphunzira panthawi yomwe akuphunzitsa. Ichi ndicho cholinga cha "okuda kuphunzitsanso okuda ";kuona mpingo ukukwera komansa kuwala kwa Yesu kukudzadzira afirika.

7. Kupachikidwa kwa Yesu sichinali chinthu chodabwitsa.Yesu ankalotsera za imfa yake, izi zatchulidwa kawiri pa mutu 9:21-27ndi 43-45.izi zikutiphunzitsa kuti Mulungu ndiye olamulira zonse zochitika.

8. Luka 15 pali mafanizo atatu, omwe ali ndi mitu yofana. Tikuona kuti Mulungu amalabadira iwo omwe ali otaika monga momwe tikuonera m'mafanizowa kuti ngakhale otaika m'modzi ndiofunikira kwambiri pamatso pa Mulungu. Onani vesi 10 ndikutsimikidzira zomwe tinenazi.

A. Luka 15:11-32. Iyi ndi nkhani ya mwana olowererandipo imalalikidwa ndi kuphunzitsidwa kawirikawiri m'mpingomu. Tikuphunziramo zinthu ziwiri zotsiyana munkhaniyi ngakhale kuti nkhaniyi ndiimodzi ndipo yogwiridzana.

B. Luka 15:11-24 ndinkhani yomwe ikufana ndi nkhani ziwiri zomwe tikuziphunzira mu ndime imeneyi yokhudzana ndi kufunikira kwa wotayika m'modzi amene wapedzeka pamaso pa Mulungu. Mwachidule timawerenga za mwana m'modzi otaika amene adapita kutali

komwe adakadzudzikako. Adakumbukira mumtima mwake,nabwerera kwa atate ake, amene adatsangalala chifukwa cha kubwerera kwa mwana waoyu. Nkhaniyi imatiphunzitsa kuti Mulungu amakondwera ndi kubwerera kwa ochimwa amene adatsokera ntatalilimo ndikulapa tchimo lake komanso kupulumutsidwa.

C. nkhani yachiwiri vesi 25-32 , ikutiphunzitsa ife za mwana wachiwiri amene adali pompo ndi bambo ake. Iye adali okwiya ndi m'mene atate ake adamulandirira ng'onowakeyu mwachimwemwe ndi mwa nsangala. Mwana wachiwiriyu ndiamene wasokera koma sadziwa dzakutsokera kwake. Akuganidza kuti ali paubale wabwino ndi Mulungu, koma sichoncho ayi ali m'mavuto adzaoneni otsadzindikira kuti Sali m'chiyanjano ndi Mulungu. Uyu ali ngati afarisi amene Yesu ankalimbana nawo. Amaganidza kuti iwo ndiolungama kupotsa aliyense. Ukuyenera kudzindikira kuti ndiwe ochimwa ndipo ukuyenera kupulumutsidwa.

9. Luka 16: 19-31 ndinkhani yomwe ikutiphunzitsa za kumwamba ndi gahena, komanso phunziro lopedza mphoto kumwamba kapena padziko lapansi pano. Tikuona kuti wachuma adatsangalala padziko lapansi pano ndipo sadamange ubale ndi Mulungu. Ndiye atamwalira adapita kumalo komwe mazunzo. Ndipo munthu otsaukayo adali mwa Mulungu, ndipo atamwalira vesi 22 ikuti m'ngelo adamtenga napita naye pachifuwa cha Abraham, amene ndimalo abwino zedi. Tikuona zinthu zofunukira pamenepa.

A. kumwamba ndi kugahena ndi malo eni eni. Kumwamba ndikwabwino koma kugahena ndi konvetsa chitsoni chifukwa ndimalo amazunzo.

B. Mazunzo akugahena adzakhala akukulirakulirabe chifukwa omwe adzakhale kumeneko adzadziwa za anthu omwe ali kumwamba ndipo adzazindikira kuti iwonso adayenera kukhala kumwamba komweko (vesi 23).

C. osangoganidzira za mphoto ya dzikolapansichifukwa ndiyosakhalitsa (25)

i. kumwamba ndimalo abwino kwambiri (25)

D. Vesi 26 munthu adzakhala kwamuyaya kumalo kumene adzatumidzidwe. Kulibe kutsamuka kugehena kupita kumwamba, kapena kuchoka kumwamba kupita kugahena.

E. Vesi 31 malemba ndiokwanira kupulumutsa munthu. Otaika adzanyodzera mfundo yakuti Yesu adauka kwa akufa.

F. Nkhani imeneyi ikutipatsa chithunzithunzi kuti m'mene moyo wathu ulili pansi pano si olingana kufunikira kwake ndi chomwe tidzakhale utatha moyo uno. Sikolakwika kukhala wachuma pamene tili padziko lapansi pano bola ngati tili paubale ndi Yesu ndikuzindikira udindo wathu ogawira chumacho kwa otsowa ndikuntchito za Mulungu.

G. palitu chitonthozo chachikulu kwa iwo amene ali mu umphawi. Moyo wapadziko lapansi ndiwakanthawi kochepa. Kumwamba kuli mphoto yokhatamira ndi yamuyaya. Pali m'ngelo amene akudikira kutenga inu kupita nanu kumwamba (Luka 16:22). Tikuyenera kukhala okhulupirika munyengo zonse zomwe ife tili.

H. Tikuphunzira kuti anthu amapita kumalo amsauso kapena komwe kuli Mulungu akamwalira. Izi sizitenga nthawi. Pamene wangomwalira nthawi yomweyo ukuitanso. 2 Akorito 5:6 ndi Ahebri akuchitira umboni zimenedzi.

9. Luka 18:1-8 tikuona za faniza lomwe likuphunzitsa za kusafoka. Mkazi wamasiye sadalore kusakhulupirika kwa oweredzayo. Adapitirira kubwerabwera pamaso pake mpaka chilungamo chitaoneka. Tipemphere kotsalekedza olo kwa dzaka zochuluka ngati kungafunike kutero.

Otsakhumudwa ndikutsiya kupemphera. Mukuyenera kupemphera ngakhale kwa dzaka zingapo mpaka Mulungu atapereka chokhumba chathu ndipo atha osakupatsa chomwe ufuna.

i. chitsanzo cha pemphero lotsalekedza ndilomwe ine ndi mkazi wanga timachita popempherera ana athu omwe si akhristu kuti apulumutsidwe. Takhala tikupemphera kwa zaka 30 ndipo tipitirirabe kutero.

10. Luka 22:14-23 ali mchipinda cha pamwamba nthawi ya pasaka, Yesu adyetsa m'gonero kapena kunena kuti adakhala ndi iye pa gome lake. Ndipo adawalamulira iwo kuti adzichita ichi pomkumbukira iye. Tiphunzira za chinthu chimenechi pamene tikhale tikuphunzira buku la 1 Akoronto.

11. Nthawi yotsilidza ya Yesu tikuona kuti adali yekhayekha ndipo amadziwa za kuzunzika kwake ndikuti ayenera apirire ndithu.

A. Ophunzira onse adamuthawa. Tikuona izi m'munda wa Gesemani pa Marko 14:32-42 adawafunsa ophunzira ake kuti asagone koma apemphere naye limodzi, koma tikunva kuti adafa ndi tulo ngakhale adawaudza kachiwiri kuti apemphere nawonso.

B. Luka 22:42 timakuwerenga pamene Yesu amafunsa kuti ngati nkutheka Mulungu alole chikhocho (mkwiyo) chimpitirire. Yesu amadziwa kuti chikhochi chidali chansauso kwambiri.Amadziwa kuopsa kwa chipsinjocho. Adadziwa m'mene adzasaukire. Komabe Yesu adatsimikidzira Mulungu kukafa pantanda, ndikuchita chifuniro chake mosawiringula. Nkhristunso ayenera kuchita zomwe Mulungu afuna, posawerengera mavuto omwe angakumane nawo, pamene achita zoterezi.

C. Luka akunena pa Luka 22:44 kuti Yesu adali muululu waukulu kuti adapemphera mpaka adagwa thukuta ngati madontho amagazi. Madotolo amanena kuti, Yesu apa adali okhumudwa kwambiri.

D. tikudziwa kuchokera mu nkhani yake, kuti Yesu amatikonda kwambiri kufikira potaya moyo wake chifukwa chaife.

12. Luka 23 tikuona za chigamulo cha Yesu kuti aphedwe ngakhala Pilato sadamupedze olakwa. Chaputalachi chimafotokozanso za kupachikidwa kwa Yesu.

A. Luka 23:39-42 ndinkhani yothchuka yomwe imatiphunzitsa zinthu zingapo zofunukira kwambiri;

i. chipulumutso sichili muubatizo. Wachifwamba adapulumutsidwayo sadabatizidwe koma ali kumwamba.

ii. Sintchito yomwe ingatipangitse ife kupulumuka. Chomwe adachita wachifwambayi, ndikungokhulupirira kuti Yesu ndi Mulungu, ndikudalira iye pachipulumutso chake, ndikuvomeredza tchimo lake,ndikupempha Yesu kuti amukhululukire. Chimodzimodzi ndiife lero; sitiyenera kugwira ntchito kuti tipulumutsidwe. Malo mwake tichite ngati wachifwambayi. Tikhulupirire kuti Yesu ndi Mulungu, ndikumupempha kuti atipulumutse kumachimo athu, ndikulapa kotero tidzapulumutsidwa.

B. Luka 23: 46 tikuona za kufa kwa Yesu. Vesi 53 tikuwerenga za ku ikidwa kwa thupi la Yesu m'manda.

13. Luka 24:1-6 patatha masiku atatu Yesu adauka kwa akufa ndipo wagonjetsa imfa. Ichi chimatchedwa chiukitso cha Yesu.

Imfa ya Yesu pamtanda idali pamene Yesu amalangika chifukwa cha machimo a mkhristu aliyense. Pantanda paja adadzudzika kopotsa kuzunzika kwa wina aliyense. Adafa pantanda paja modzipereka chifukwa cha akhristu onse. Padali pantanda pomwepo pamene Yesu adagonjetsa satana. Imfa ya Yesu ndichifukwa chomwe akhristu sayeneranso kupita kugehena kukazunzikanso chifukwa cha machimo awo. Izi zili chomwechi chifukwa Mulungu adavomeredza chilango cha opanda bangayo Yesu ngati dipo la tchimo. Anthu onse amene amamwalira atsali a khristu amapita ku gahena kuti akalipire dipo la machimo awo.

Kuuka kwa Yesu ndichitsimikidzo chamfundo yakuti wagonjetsa imfa pamene adali pantandapo. Kuuka kwa Yesu kumatsimikidzira kuti m'khristu wina aliyense wagonjetsa imfa ya udzimu ndipo adzapita kumwamba m'malo mwa kugahena.

## ZIPHUNZITSO ZA BUKU LA YOHANE

Buku lofunikira kwambiri m'Baibulo lidalembedwa ndi Mtumwi Yohane. Mtumwi amatanthaudza amene watumidwa ndikuitanidwa kukhala mtumwi; munthu amene adaona Yesu ndi maso ake. Aroma 1:1 tikunva zoti Yesu adaitanidwa ndi Mulungu kukhala mtumwi. Buku la Yohane limaonetsa monveka bwino kuti Yesu ndi Mulungu. Tiphunzira zambiri zokhudza kuti Yesu kuti ndiye yani (Mulungu) mubuku la Yohane. Buku la Yohane limatsiyana kwambiri ndi mabuku atatu a uthenga wabwino.

1.Yohane 1:1-5ndimavesi ofunikira kwambiri. Yohane akutiudza kuti Mau (Yesu) ndi Mulungu. Kuti Yesu ali ndizikhalidwe zonse za Mulungukuphatikidzapo umuyaya wake komanso ndiiye Mlengi wathu. Moyo wathu uli mwa iye, ndipo amadziwika kuti ndiye kuunika ndipo iye wagonjetsa imfa (nditchimo).

A. Mfunso lofunukira kwambiri m'moyo uno ndilakuti "Kodi Yesu Christu ndindani" kodi ndi munthu wamba kwa inu kapenaso ndi Mulungu? Pokhala nkhristu uyenera kukhulupirira kuti, iye ndi Mulungu ndipo tikuyenera kutsata iye. Izi zikutanthaudza chiyani? Zikutanthaudza kuti tiyenera kunvera iye kukonda iye ndikutumikira iye. Khulupirirani kuti Yesu ndi Mulungu, ukuyenera kumuitana iye kuti akhale Mbuye wako ndikulapa machismo ako pamaso pake.

B. Yohane 1:10-13 akutiudza kuti dziko lapansi-anthu amakana kulemekedza amene adawalenga. Akadali kulimbana ndi Yesu Khristu. Yesaya 1:3 timanva kuti ng'ombe ngakhale abulu amadziwa mbuyewao, koma munthu nthawi zambiri amaoneka kuti sadziwa zoti Mulungu ndiye Mbuyewawo. Izi ndizoona masiku alerowa.

C. vesi 12 akhristu amakhala ana a Mulungu, iye amawapanga iwo kukhala ana ake. Ndife ana ake kotero kuti tili ndi ufulu komanso zabwino zonse monga m'gwiridzano komansochitsamaliro cha Mulungu.

D. Vesi 13 muli nkhani ya kubadwa mwa Mzimu- kubadwa mwa sopano. Uku ndiko kubadwa kuchokera kumwamba, ndipo akhristu onse akuyenera kubadwa mwatsopano. Ichi ndi chauzimu chochokera kwa Mulungu chotsiyana ndikubadwa kwa kuthupi

E. Vesi 14 Mulungu akukhala pamodzi ndi munthu, chomwe chili chinthu chodabwitsa kwambiri. Adatsiya ulemerero wakumwamba ndikubwera kudzakhala nafe. Adadzunzika ndikuyetsedwa monga ngati ife.

2. Yohane 2:1-11 chozizwitsa choyamba kudali kusanduliza madzi kukhala vinyo-Yesu akuonetsa kukhudzika ndizonse zomwe zimachitika ndianthu ake. M'chifukwa ninji Yesu

amachita zozizwitsa? Cholinga chake kunali kulimbikitsa utumiki wake. Chifukwa china ndichakuti Yesu adali wachifundo ndi anthu ndipo amasangalala pothandidza iwo.

A. Yohane 2:12-17 Yesu akonza kachitsi monga momwe Nehemiya 13:8 Nehemiya adachita chomwechonso. Phunziro kwa ife ndilakuti timapemphera Mulungu mutchalitchi tiyetsetse kuti otsakhulupirira atsaononge chipembedzo cha Yehova. Tionetsese kuti oyankhula mumpingo akhale anthu okhulupirira okha basi. Tisalole munthu kuti ayankhule mumpingo chifukwa adatipatsapo ndalama. Olalika mu mpingo mwathu akhale okhawo amene ndiokhulupirika pamau a Mulungu.

B.Muvesi 18-22 adawapatsa chidzindikiro chomwe palibe adachinvetsa mpaka nthawi yakukwaniritsa kwake. Adalotsera za imfa ndi kuukakwake.

3. Mutu 3 werengani mavesi 1-17.

A. Yesu adadziwa mtima wa Nikodemo chifukwa Nikodemo adali oyimirira anthu onse. Adali chitsanzo cha ena. Adafuna chikwaniritso cha Mzimu m'moyo mwake. Sadafune kuvomeredza yankho la Mulungu.

B. Vesi 1-2 tikuudzidwa kuti Nikodemo adali olamula wachuma amene adabwera kwa Yesu mwachinsisi. Amafuna mayankho kuchokera kwa Yesu chifukwa Yesu adali otsiyana ndi anthu ena komabe sadali onkozeka kuvomeledza zomwe Yesu amayankhula ndi iye. Vesi 13 Nikodemo akuyankhula ndi Yesu Khristu. Chomwe tiyenera kuchita ndiko kuvomeredza Yesu otsati kumatsutsana ndi Mulungu.

C. vesi 3-5 kubadwa mwa tsopano. Akhristu onse ndi obadwa mwatsopano. Zikutanthaudza kuti timabadwa mwa Mzimu kuchokera kwa Mulungu. Koyamba timabadwa kuthupi, kuchokera mwa amayi.

D. Vesi 5 tikunva za kubadwa kwa madzi ndi mzimu. Madzi akutanthaudza Mau a Mulungu, Mzimu utanthaudza umboni wa Mulungu=Mzimu Woyera mwa ife. Mwanjira ina Baibulo ndi Mzimu Woyera zimagwira ntchito limodzi potipanga ife kukhala akhristu.

E. vesi 6 galu sabala mbuzi. Mwanjira ina thupi (tchimo) limatulutsa munthu ochimwa. Ndipo Mzimu wa Mulungu umabala munthu wa uzimu- moyo wa tsopano. Ndipo moyo okonda Mulungu umachokera mwa munthu otembenuka mtima. Pakhale ndithu kusintha mwa iye olengedwa wa tsopano ngakhale pachiyambi zimachitika mwapang'onopang'ono.

F. Vesi 14-15. Sintchito yomwe timapulumutsidwa nayo, koma pakuyang'ana kwa Mulungu ndi chikhulupiriro.

G. Tiyeni tione Yohane 3:16 imene ndi vesi yotchuka kwambiri m'baibulo. Anthu samanvetsetsa bwino zachikondi cha Mulungu. Tiyeni tiyankhulepo za chikondi cha Mulungu.

i. Mau oti kukhulupirira tingawatanthaudzire muvesiyi kuti yense amene ali ndi chikhulupiriro mwa Yesu ndi opulumutsidwa. Tanthauzo la chikhulupiriro ndikukhulupirira chinthu chotsaoneka ndi maso. Timakhulupirira mwa Mulungu ngakhale sitimuona iye.

ii. chikondi cha Mulungu chilibe malire Aefeso 3:17-19. Chikondi cha Mulungu chilibe mathero.

iii. Chikondi cha Mulungu ndi chikondi chopirira. Chimapanga Mulungu kuchitapo Kanthu. Mulungu Atate adapereka mwana wake kudziko lapansi, ndipo Yesu adachoka kumwamba natsiya ulemerero wake ndikuzunzika pansi pano. Chikondi chenicheni chimapirira msautso.

iv. Onani nkhani ya Hoseya ndikuona kuti chikondi chimapirira. Tikuona kufanana kwakukulu Kwa chikondi cha Hoseya kwa mkazi wake Goma ndi chikondi cha Mulungu ndi anthu ake.

a. Hoseya adali bambo wabwino kwambiri. Ubwino umabala chilungamo chocho Mulungu ndiye ochitira ubwino.

b. Hoseya adali ndi mkazi wosakhulupirika amene amatsiya Hoseya nakhala ndi amuna ena. Chimodzimodzi anthu a Mulungu amene amachoka pamatso pa Mulungu napita Kwa milungu ina. Komabe Hoseya mounikiridwa ndi Mulungu adamupatsa chakudya mkazi otereyu monganso Mulungu amene saleka kusamarira anthu ake ngakhale nthawi zonse amachoka pamaso pake. Hoseya adamuombola mkaziyu atagulitsidwa ngati kapolo monga momwe Yesu adatiombolera ife kuukapolo wa tchimo.

c. Chikondi cha Mulungu monganso cha Hoseya ndichofunafuna. Mulungu amatifunafuna ife ngakhale tiliochimwa. Amatipulumutsa ife ku chinthu chotiyenera ndiuchimo wathuwu ndiye gehena.

H. Tikaphatikidza vesi 16 mpaka 17 ya Yohane mutu wa 3 tikuona nkhani yotheratu ya chikondi cha Mulungu. Tikuona kuti Yesu adabwera kudziko lapansi kutipulumutsa ife kotero chipulumutso chilipo kudzera mwa Iye.

4. Yohane 3:18-21 ndichifukwa ninji anthu safuna kukhulupirira Yesu ndikuti apulumutsidwe. Anthu ambiri akukana Yesu chifukwa akutsangalala kukhala m'moyo wa uchimo. Osakhulupirira ambiri amaganidza kuti kukhala nkhristu zimakuchotsa muchitsangalalo chenicheni. Ndiye amaganidza kuti ndi nthawi yao kuti asangalale kenako kumapeto kwake adzakhale mkhristu. Vuto lake limakhala lakuti atha kumwalira mwachangu. Mulungu amalolera kuti awaumitse mitima yao pa machimo awo kuti adzawawerudze mumphulupulu yao. Kumbukirani Farao.

B. Masalmo 10:4 akunena za kunyada ngati chimodzi mwa zifukwa zimene anthu amakanira Yesu. Kunyada kumapangitsa anthu kukana Mulungu chifukwa timafuna kupanga zinthu mwanjira yathu osati monga Mulungu afunira. Ndidzonyadiritsa kwambiri kulandira chipulumutso choperekedwa kwaulele; koma ife m'malo mwake timafunafuna chipulumutso chogula ndi ntchito zathu.

5. Vesi 22-36 kawiri tikuona kudzichepetsa kwa Yohane ndi kukwedzeka kwa Yesu khristu vesi 22-30 tikunva kuti Yohane adali wankulu ndithu ndipo adali ndi ophunzira Yesu asanabwere. Koma Yohane adali otsangalala kupereka utumiki wake ku utumiki wa Yesu. Kodi ndinu okonzeka kutula udindo wanu kwa ena pamene nthawi yanu yapampando yatha? Yohane adaponya maso ake pa Yesu.

A. Vesi 31-36 akutsindikidza maitanidwe a Yesu. Yesu yekha adachokera kwa Mulungu atanyamula ulamuliro wa Mulungu chifukwa iye ndi Mulungu. Ngati ukana Yesu, ukukana moyo osatha ndikutsankha nkwiyo wa Mulungu. Onani choona chake kuchokera mu vesi 36.

6. Mutu 4:1-14 tikuona za umunthu wa Yesu. Motani? Vesi 5-7 ikunena kuti Iye adatopa komanso adanva luzi. Munthawiyi iye adali ku Samariya kumene Ayuda samapitako chifukwa anali pa udani ndi akuSamaliyawa chifukwa adawalanda malo awo. Popita ku

Samaliya Yesu akuonetsa kuti chipulumutso si cha Ayuda okha. Chivumbulutso 5:9 akuti iye adabwera kupulumutsa ntundu uli onse wa dziko lapansi.

A. dziwani kuti monga m'munda wa Edeni, Mulungu ndiamene adayamba kuyankhula kwa mkazi. Mulungu ndi amene amayamba kuyankhula pofuna kumanga ubale.

B. Vesi 10 Yesu akupereka kwa mzimayiyu Madzi a moyo-kodi ichi ndi chiyani? Mundime izi akuthandaudza kuti madzi ndi chinthunzithunzi cha Moyo wotsatha. Chisomo cha Mulungu chili ngati kasupe amene amapereka madzi amoyo. Mulungu ndi ofunikira ku moyo wathu. Amatipatsa madzi a moyo/moyo otsatha.

Nthawi zambiri chipangano cha kale chakhala chikunena za madzi a moyo, onani Yesaya 12:3, Masalmo 42:1 ndi Yeremiya 2:13.

7. Vesi 23-24 chinthu chimodzi chomwe Mulungu amafuna kwa munthu. Amafuna ife kumupembedza iye muuzimu ndi muchoonadi. Cholinga chenicheni chimene munthu adalengedwera ndiko kupembedza Mulungu ndi kukondwera mwa iye nthawi zonse. Tidalengedwa ndi cholinga chopembedza Mulungu. Dziwani kuti Mulungu amakhumba kupembedza kwathu. Safuna zambiri kuchookera kwa ife koma kum'pembedza Iye.

A. Buku la Yohane likutionetsa zinthu zitatu zofunikira pa chipembedzo chovomeredzeka.

i. Mutu 3 vesi 7 ikuti tiyenera kubadwa mwa tsopano. Otsapulumutsidwa sangathe kupembedza Mulungu. Munthu angapembedze bwanji Mulungu ngati sam'khulupirira Iye?

ii. Mutu 3 vesi 14 ikuti Yesu akwezedwe pamwamba pa zonse. Tiyenera kukwedza mau ake-Baibulo.

ii. Mutu 4 vesi 23 ikuti tiyenera kumpembedza Iye mumzimu ndi muchoonadi. Zikutanthaudza chiyani?

a. Kupembedza= timanena za zeni zeni za Mulungu. Mulungu akuyenera kupembedza kwathu.

b. Kupembedza mumzimu= kupembedza koyenera kumachitika pamene Mzimu wathu omwe umatitsiyanitsa ndi zolengedwa zonse omwe umalumikidzana ndi Mulungu komanso gawo lomwe Mulungu amaliyankhula.

c. Kupembedza muchoonadi =timamufikira Mulungu moona ndi mtima wathu wonse.

Timamupembedza Mulungu mosogozedwa ndi Mau ake. Ndipo zigawo zikuluzikulu ndi chiyamiko, pemphero, ndi kulalikira Mau ake- Baibulo.

Tingamupembedze Mulungu kudzera mwa Yesu yekha basi, onani Yohane 14:6.

8. Vesi 25-42

A. Muvesi 25-26 Yesu akudziulula yekha kuti ndiye Mulungu Mesiya.

B. Mutu 4:27-30 ophunzira anali odabwa chifukwa Ayuda samayankhula ndi Asamaliya. Sikumaloledwa kunena ndi mzimayi pa gulu. Malamulo onsewa adali okonzedwa ndi munthu osati Mulungu ayi. Yesu adawaonetsa anthuwa kuti ndikoyenera kuyankhula ndi Asamaliya komanso mzimayi nthawi ili yonse. M'moyo uno mauwa akutanthaudza kuti tikuyenera kuyankhula ndi otsakhulupirira, otsawatsala ayi.

i. Ndikukhulupirira kuti chifukwa chimene chidamupulumutsa mzimayiyu chidali chakuti Yesu adamudziwa kuti adzakhala okhulupirika ndikuchita chomwe tonse timachita pamene tatembenuka mtima; adapita nakanena kwa ena zokhudzana ndi Yesu. Adachita ntchito ya mulaliki.

C. Yesu anabwera kupulumutsa anthu onse osati Ayuda okha, ndipo izi zinapangitsa Ayuda kukwiya ndi Yesu. Ndipo Ayuda adafuna kumupha iye pamene adayankhula izi. Onani Luka 4:26-30. Apa Yesu adawaudza kuti monga Eliya adapita ku kudziko lachilendo kukapulumutsa anthu achilendo chimodzimodzi Yesu kuti anadza kudzapulumutsa anthu amitundu yonse ndipo otsati Ayuda okha.

D. Vesi 31-34 chimwemwe chenicheni chimabwera pakuchita chifuniro cha Mulungu. Ngati sitichita chifuniro cha Mulungu, nanga tikuchita chifuniro chandani? Timachita chifuniro cha Mulungu kapena chifuniro cha machimo athu. Koma tikuyenera kuchita chifuniro cha Mulungu. Timadziwa bwanji chifuniro cha Mulungu? Malemba amatiudza ife ndiponso timapemphera ndikufunsa Mulungu kutiululira chifuniro chake ndipo timaphunzira za mphatso zomwe Mulungu amatipasa.

E. Mutu 4:35-38 pali lamulo lotchuka kwambiri. Limene ndi kufalitsa uthenga.

F. Vesi 39-42 mkaziyu adafalitsa mau a Yesu ndipo izi zinapangitsa ena kubwera kwa Yesu ndikupedza chipulumutso. Mkaziyu adali mlaliki weniweni.

9. Mutu 5 ukuyamba ndikuyankhula za sabata.

A. Vesi 1-19 Yesu adachilitsa munthu patsiku la sabata. Ndipo izi zidapangitsa akulu a Ayuda kupsa mtima. Ndipo tidakambirana za sabata mbuku la Mateyu.

B.Vesi 17-23 kuchokera nthawi imeneyi kupita nsogolo Ayuda anada Yesu nafuna kumupha iye. Apa tikuona kuti Yesu ndi Mulungu Atate ndi amodzi chifukwa Yesu ndi Mulungunso. Tikuona kuti Yesu ali ndi ulamuliro. Ayenera matamando. Iye ndi Atate ndi amodzi.

C. Vesi 18 Ayuda akukana zimenezi ndipo akufunafuna kumupha iye. Ndizoona kuti lero anthu amakana kumulandira Yesu monga m'mene iya alili; amafunafuna kupanga kamulungu kofana ndi zolinga zao.

D. Vesi 24-29 ikuphunzitsa kwambiri za ulamuliro wa Yesu. Tikuona apa kuti Yesu ali ndi ulamuliro otipulumutsa ife ndipo timapulumutsidwa ndi (vesi 24) chikhulupiriro pa Yesu.

i. umu muli moyo komanso imfa ndipo ambiri sakhulupirira ichi. Pali ziphunzitso zitatu pamenepa.

a. imfa simathero; onani Gen25:8 1Atesalonika 4:16 ndi Ahebri 11:35

b. pali malo awiri ofikira ukatha moyo uno. Gahena onani Chiv.21:8 ndi Kumwamba onani Chiv.21:4

c. kumene mudzapite zizatengera ndi ubale omwe muli nao ndi Yesu.

E. kodi Mulungu adzapereka mwayi wachipulumutso kachiwiri? Ayi. Malamulo adawapanga kale kuti palibenso kutembenuka mtima pamene wangomwalira. Kumbukirani Luka 16:19-26 pazamalamulo ena omwe anena zokhuzana ndi kumwamba komanso kugahena. Kumbukirani kuti limodzi mwa makhalidwe a Mulungu ndi kusasintha= sasintha Mulungu.

F. Yohane 5:39-44 Ayuda amagwiritsa ntchito mau a Mulungu motsayenera. Vesi 39 ikuti cholinga chamalemba ndi kulodzera anthu kwa Yesu. Ayuda amayetsa kuti Baibulo limanene za ilo lokha. Adaliphunzira ilo pazolinga zao. Adatenga Yesu ngati munthu wamba osati Mulungu; kodi inu mumachitanso chimodzimodzi? Amapembedza Baibulo kutsiya yemwe adalilemba. Amangotsindikidza mbali zina za Baibulo. Amaphunzira za Baibulo osati za Mulungu. Amaganidza kuti kulowedza Baibulo zingawapulumutse.

Amamva bwino pamene anali kusunga malamulo koma samadziwa kuti chikristu ndi ubale wabwino pakati pa ife ndi Yesu Khristu. Sitingapulumutsidwe chifukwa chomvera malamulo.

G. Vesi 45-47 Yesu akunena kuti ndi mau am'Baibulo amene amadzudzula anthu. Anthu adanyodza ziphunzitso za Mulungu monga m'mene Mose adaziphunzitsira ndipo iwo awerudzidwa kale.

10. Mutu 6 vesi 1-14 tikuona za chozizwitsa chimene chikupedzeka m'mabuku onse a Uthenga wa Bwino. Panthawiyi Yesu anali atakopa omutsatira ambiri. Anthu amkamutsatira Yesu chifukwa amafuna chinachake kwa iye.

A. Anthuwa adali ndi chotsowa- adali ndi njala ya kuthupi. Adadziwa zotsowa zawo. Padalibe njira yothetsera vutoli kupatula kupita ndi vutoli kwa Yesu. Yesu ndiokwanira kukwaniritsa chotsowa cha anthuwa monga nkhaniyi inena kuti adadyetsa khamu lonse.

B. Yohane 6:30-35 ndi 48 and 51 akunena za chotsowa china cha anthu, njala ya ntundu wina. Njala ya uzimu. Afunikira chipulumutso. Akuyenera kuzindikira za chotsowa chimenechi kutinso palibe munthu amene angakwaniritse chotsowa chimenechi. Ayenera kuyang'ana kwa Yesu kuti akwaniritse chotsowa chimenechi chauzimu pakuti chosowa cha uzimuchi chingakwaniritsidwe ndi Yesu basi. Pamene titembenukira kwa iye, adzakwaniritsa chotsowa chimenechi. Iye ndiokwanira kukwaniritsa chotsowa chimenechi. Monga m'mene amatipatsira mkate wakuthupi, iye ndi mkate wathu wa wamoyo.

i. Timafunikira chakudya chakuthupi kuti tikhale ndi moyo. Tisowekeranso chakudya cha uzimu tsiku nditsiku kuti tikhale ndi moyo.

ii. Tikufunikira kukula mwauzimu kupyolera munkate wamoyowu. Ndipo izi zimatheka pamene tipemphera ndikuwerenga Baibulo tsiku ndi tsiku. Kumbukirani ambiri adamwalira chifukwa cha kuwerenga Baibulo. Kodi mumaliwerenga tsiku ndi tsiku?

iii. Vesi 48 Yesu akuwakumbutsa anthu, kuti Mulungu adapeleka mkate wakuthupi m'chipululu muja anthu nadya komanso napedza mphamvu koma pamapeto pake iwo adafa.

iv. Vesi 51 kenako Yesu akuyankhula za mkate wa uzimu umene uzatipange ife kukhalako mpaka kalekale mwauzimu. Uwu umaperekedwa ndi Mulungu ndipo ndiokhadzikika kusiyana ndi mana muchipululu muja.

v. kumapeto kwa vesi 51 Yesu akunena za nsembe yomwe adzapereke ndi thupi lake.

C. Tsopano tiyeni tione mbali yosiliza ya vesi 37 imene ikunena kuti Mulungu azalandira onse akubwera kwa iye ndipo sadzataya ngakhale m'modzi wa iwo akufuna Iye.

E. Tiyeni tione Yohane 6:40 momwe tikuonamo za lonjezo limene tinganene kuti = lonjezo la moyo wosatha.

F. tione mofatsirira mutu 6:41-47 tikunva kuti izi zinapangitsa Ayuda kumuda Iye chifukwa anati "Ndine mkate wa moyo wochokera kumwamba". Yohane 6:42 iwo amati "kodi uyu

Yesu simwana wa Yosefe, amene abambo ndi mayi wake tiwaziwa bwino? Nanga bwanji anena kuti ndatsika kuchokera kumwamba.”

G. Yohane 6:43 Yesu adawayankha nati “musang’ung’udze wina ndi mnzache”. Adawaudza iwo Malamulo oyenera kuti munthu afike pamaso pa Mulungu mvesi 44-47. Anthu sakondwera kulandira Mulungu monga m’mene iye aliri. Timafuna kumusintha iye, ndipo m’mene ife timaganidzira, timafunanso Mulungu akhale chimodzimodzi. Koma vuto ndilakuti sangakhale wam’ngwiro monga m’mene Iye aliri komanso sangakhale Mulungu.

11. Yohane 6:51-59. Ndime imeneyi imalakwitsidwa ndi anthu ena omwe amaganidza kuti chikristu ndichipembedzo cha anthu okudya anthu anzawo. Koma izi zimatanthaudza phwando la kuuzimu. Mwauzimu timamutenga Yesu muthupi lathu ndipo ngati chakudya chomwe chagayidwa Iye amafikira mbali iliyonse yathupi lathu nakhazikika m’menemo.

A. Yohane 6:66-68 timaphunziramo kuti otsala ndi Yesu amakhala ochepa komabe adzakhala ndi ake akhulupirika. Omutsatira ambiri amagwa mphwayi nabwerera akakumana ndi mavuto panjira yao; kodi ndichimodzimodzi ndi inunso?

B. Yohane 6:69-71 tikuwerenga kuti Petro adayamkha za kubwerera kwa anthu kutsata Yesu. Petro akukhalabe okhulupirika, koma Yesu akupenekerabe kuti ophunzira m’modzi adzampereka Iye, ndipo tikudziwa kuti ophunzira ameneyu ndi Yudasi.

12. Yohane 7:53-8:11. Nkhaniyi sidapedzeke mu zolemba zoyamba koma nkhaniyi ndiyofana ndi zochitika zonse za mubukuli. Muli zinthu zofunikira kwa ife.

A. Chigololo chimachitikanso ndi mwamuna. Ndichifukwa ninji mkazi yekha amalangidwa akagwidwa akuchita chigololo.

B. tikuyenera kukumbukira vesi 7 pamene tifuna kupereka chilango kwa munthu. Tilange munthu ngati chilungamo chifuna kutero; osati chifukwa cha zikhumbitso za munthu kapena zitsangalalo zake. Ili ndilamulo labwino kutsatira pofuna kulanga mwana. Kumbukirani kuti ifenso tili ndi zambiri zomwe tiyenera kulangidwa nazo. Ayuda anachita izi ndi cholinga chofuna kumupedzera Yesu zifukwa otsati mwachilungamo.

13. mutu 8:12-59.

A. Yesu adayankhula kuti Iye ndi Mulungu. Afarisi muvesi 13 akunena kuti Yesu ndi onama ndipo izi zidapangitsa Yesu kuwadzuzula molimba.

i. Vesi 15 powadzudzula kuti iwo amawerudza monga mwa thupi.

ii. Vesi 19 potsaziwa Atate. Yesaya 1:3 amaphunzitsa zonga zomwezi.

iii. Vesi 21 ndi 24 akuonongeka muuchimo wawo.

iv. Vesi 23 powadzudzula kuti iwo ndi adziko lapansi.

v.Vesi 34 kuti ndiwo akapolo a tchimo.

vi. Vesi 44kuti ndiwo ana a Satana. Aliyense ndi mwana wa Satana kapena mwana wa Mulungu. Tisadapulumusidwe timakhala ana a satana.

B. izi zinali zoona koma ngakhale zinali chomwechi zinapangitsa Ayuda kunyatsidwa ndi Yesu. Tiyeni tione zomwe iwo adachita potsatira zomwe Yesu adanena.

i. Vesi 41 ananzuzula iye kuti anabadwa motsayenera.

ii. Vesi 48 anamuzuzula Yesu kuti ndiye M'samaliya osati muYuda ndipo paichi iye ndi njerekezi.

C. Vesi 59 ikunena za momwe adayetserera kumupha Iye, chifukwa izi sizikanatheka popedza siinali mphamvu yao kuchita izi.

14.mutu 9:1 tikuona kuti Yesu ataopsezedwa ndi imfa akupita kukachita ntchito ya chifundo. Ndi angati a ife omwe tingachite motere? Zikuonetsa chikondi chopotsa chomwe Yesu ali nawo pa ife.

A. Vesi 2-3 tikunvapo za ganizo lolakwika limene limati tchimo linalake limamupangitsa munthu kukhala m'mavuto. Ili linali vuto lomwe lidalipo munthawi ya Baibulo mbuyomo. leronso izi zikupitirirabe. Onani Luka 13:1-5 kuti mutsimikidze kuti izi sizoona.

B. Ngakhale kuti izi ndi zoona zoti mavuto onsewa ndi gwero latchimo; vuto lanulo sikuti layambika chifukwa cha tchimo lina lake lomwe munalichitapo ngakhale kuti nthawi zina zinthu zimatha kutero. Aneneri onyenga amatero powaudza anthu kuti mavuto awo adza chifukwa cha chinachake chomwe adachichita nthawi ina yake. Ndinkhaza kumuudza munthu kuti akuvutika chifukwa cha zomwe adachita nthawi ya m'mbuyomo. Ngakhale izi zitakhala zoona. Mwachitsanzo, ngati munthu akumwalira chifukwa cha Edzi yomwe inadza pochita tchimo la chigololo, sichanzeru kuyenjedzera chisoni chake pomuudza kuti akuvutika chifukwa cha ntchimo lomwe adalichita m'mbuyomo.

C. Nthenda zina zimayambika chifukwa cha tchimo la wina. Chitsanzo cha izi ndi Edzi kapena vuto la kuononga kwa kachaso kwa mwana yemwe mai wake adali kumwa kachaso iye asanabadwe.

15. Mutu 10 tikuona Yesu akuonetsedwa ngati m'busa wabwino. Mbusa yemwe amasamalira nkhosa zake. Adayankhula kuti iye ndi njira ya chipulumutso ndipo kuti ndiye mbusa amene adzataye moyo wake kuti apulumutse anthu ake.

A. Vesi 27-29 ndichitonthozo chachikulu kwa akhristu onse. Yesu akuti sadzalola ana ake kuti atayike. Mwanjira ina ngati wapulumutsidwa udzakhalabe wopulumutsidwa mpaka kale. Ichi ndichitonthozo chachikulu zedi.

B. ichinso choti Yesu angathe kupulumutsa anthu chinapangitsa Ayuda kumfunafuna iye kuti amuponye mundende, vesi 39. Kachiwirinso adawazemba iwo chifukwa adalibe mphamvu zomumangira. Akadamumanga iye ngati akadawapatsa mphamvu kuti atero.

C. Vesi 19-21 ndi 42 ikunena za kugawanika kwa Ayuda ndiponso kuti ambiri adamkhulupirira Iye.

16. Mutu 11:1-44 pali nkhani ya kumwalira kwa Lazalo, kuikidwa kwake ndikuukitsidwa kwa akufa ndi Yesu.

A. nkhaniyi imaonetsa kuti Yesu ali ndi mphamvu pakati pa moyo ndi imfa kotero Iye ndi Mulungu chifukwa Mulungu yekha ndiyemwe ali ndimphavu zotere. Vesi 15 cholinga cha nkhaniyi ndikupanga anthu kuti akhulupilire.

B. Vesi 35 ikuti Yesu adalira. Ndichifukwa chani Iye analira? Mwazonse Iye anadziwa kuti pamapeto pake Lazalo adzauka nakahala ndi moyo.

i. adaonetsa chikondi chake kwa anthu pamene amalira nawo pamodzi.

ii. adaonetsa kuti sivuto anthu kulirira okondedwa awo akamwalira, ngakhale kuti wokondedwayo wapita kumwamba. Maulaliki ambiri akhala akulalikidwa mopotoka kuti sitiyenera kulirira okondedwa athu omwe amwalira chifukwa iwo ali kumwamba.

iii. Ena amanena kuti analira chifukwa chakuipa kwa imfa  ndi chisoni pa imfa.

C. Vesi 4 ndi 40 cholinga china cha nkhaniyi ndikufuna kuonetsera ulemerero wa Yesu.

D. Vesi 45 ikunena kuti ena anayamba kukhulupirira Yesu chifukwa anautsa Lazalo kwa akufa. Ena sanalabadire za chimene Yesu adachita koma anapitilidza kuchitirabe chipongwe Yesu kuti Iye si Mulungu. Vesi 45-53 ikunena kuti akhunguwa adakonza chiwembu kuti aphe Yesu.

17. Mutu 12:1-8 ndinkhani ya Mariya yemwe adazoza mapazi a Yesu ndi mafuta amtengo wa patali. Uku kunali kulemekedza Yesu pa chakudya chomwe iye anapatsidwa.

A. Vesi 9-11 ikunena za momwe anthu adayambira kukhulupirira Yesu chifukwa chodzutsa Lazalo kwa akufa. Izi zidapangitsa akulu ansembe kufuna kumupha Iye.

B. Vesi 12-19 ikunena zamomwe Yesu mwachipambano adalowera mu Yerusalemu atakwera pa bulu, monga m'mene zinalosedwera ndi Zakariya 9:9. Mpingo umatsangalala lamulungu isadafike pasaka (isita) chifukwa cha vesi 13, ngati Lamulungu la kanjedza. Luka 19:33-38 timanva kuti khamu lalikulu linamulandira Yesu ngati Mgonjesi tsiku Lamulungu ndipo Lachiwiri adafuna kumupha Iye. Anthu amakukonda mukamphindi ndipo nthawi yochepa amakutembenukira. Ndi Mulungu Yekha amene ndiokhulupirika.

18. Mutu 13-17 ndimavesi odziwika bwino onena nkhani ya kuchipinda cha pamwamba. Asadapachikidwe utsiku wake Yesu adakumana ndi ophunzira ake muchipinda chapamwamba nawaphunzitsa iwo za udindo wao watsopano ndi zabwino zomwe adzapedze ngati chotsatira cha imfa yake, mwanjira ina, iyi ndi nthawi yomwe ophunzirawa akuyenera kukula ndikusenza udindo pothandizidwa ndi Mzimu Woyera poyamba ndi kufaritsa chikhristu kudziko lonse lapansi. Ndipo Machitidwe a Atumwi amati iwo adachita momwemo.

A. Mutu 13:3-20 akunena zakuti Yesu asuka mapazi awophunzira ake. Muli zambiri zoti ziphunzilidwe zokhudza kudzichepetsa pamene Mulungu mwini akutsuka mapadzi a anthu otsayenera. Titsanzire Yesu pamene tikutumikira modzichepetsa. Sitinalamulidwe kutsuka mapadzi, kumbukirani kuti ichi chidali chikhalidwe munthawi ya Baibulo.

B. Muvesi 10 Yesu akuulula kuti m'modzi mwa ophunzira ake ndiamene adzamupereke.

C. Vesi 16 ikutiphunzitsa kuti utsogoleri mumpingo ndiofunikira kwambiri. Mamembala a mumpingo sangakhwime ndikupita patsogolo ngati alibe atsogoleri abwino. Ndipo ichi ndichifukwa tabweretsa phunziro ili la Afirika kuphunzitsa Afirika nzake. Atsogoleri mokhulupirika aphunzitse Mau a Mulungu kuti mamembala awo akhwime ndi kupita pasogolo muuzimu. Kumbukirani kuti mphuzitsi akuyenera kuphunzira kwambiri kupotsa wophunzitsidwa.

i. mavesi 34-35 Yesu akupereka lamulo lamomwe tiyenera kukonderana wina ndi nzake. Onani Marko 12:31 kuti muone kufunikira kwa chinthuchi.

ii. mavesi 37-38 akukamba za kuzitama kwa Petro ndi chilimbikitso chomwe anali nacho, ndi zomwe Yesu adanena za kugwa kwa Petro pamapeto pake. Iyi ndinkhani yotchuka kwambiri. Tidzitsamala ponyada.

19 Mutu 14:1-4 Yesu akupitiridza kuwakonzekeretsa ophunzira ake pa imfa yomwe ikumfikira, ndikuwaphunzitsa iwo uthenga wa chitonthozo chachikulu.

A.Vesi 1ikuwaudza iwo kukhulupirira Mulungu ndikutonthozedwa mwa Iye.

B. Vesi 2 Yesu akuudza iwo kuti Kumwamba malo aliko ambiri, ndipo Iye akupita kukawakonzera iwo malo kuti kuli Iye iwonso akakhaleko.

C. Mavesi 3-4 Yesu akuwaudza kuti adzabweranso kudzatenga iwo kupita nawo Kumwamba. Uthengawu umkafuna kuthandidzira iwo kutonthodzeka m'matsiku amsautso amene adali kubwera patsogolo pao. Izinso zititonthodze ife chifukwa uthengawu ndi wa a khristu onse.

D. tikufika ku vesi 5-6 kuziphunzitso zofunikira kwambiri. Funso ndilakuti umakhulupirira Yesu yekha? Yohane 14:6 ikuti "Ine ndine njira choonadi ndi moyo. Palibe angapite kwa Atate otsadzera mwa Ine."

i. Nkhristu ndiamene amaika chikhulupiriro chake ndikudalira konse mwa Yesu Khristu Yekha basi. Chikhristu ndichipembezo chasankho kwambiri. Mulungu wathu ndi Mulungu wa msanje. Sagawana ulemerero wake ndi munthu aliyense, onani Yesaya 48:11. Sitiyenera kuchita chilichonse ndi asing'anga komanso sitiyenera kukhulupirira zamasenga zao.

ii. Mipingo yambiri padziko lapansi imaphunzitsa kuti anthu akhalidwe labwino adzapita kumwamba potsawerengera zomwe amakhulupirira. Tisalole ziphunzitso zotere kulowa mumpingo mwathu. Baibulo limatsindikidza kuti njira yokhayo yopitira kumwamba, ndi kupyorera pa chikhulupirora mwa Yesu Khristu basi.

E. Yesu mu vesi 9 akuyankhula kuti Iye ndi Atate ndi amodzi, izi zikutithandizira kunvetsetsa Utatu wa Mulungu. Mwanjira ina Yesu ndi Mulungu.

F. Mutu 14:12-14 ndimavesi amene anthu samawanvetsetsa.

i. Yesu akunena mu vesi 12 kuti mphamvu ya uzimu idzakula mwa ophunzira ake Iye akadzapita kumwamba chifukwa Yesu adangolalikira mu Israeli mokha ndipo adangofikira anthu ochepa ndi uthenga wake. Ophunzira ake adzapatsidwa mphamvu ya Mzimu Woyera yomwe idzathandidzire kuti ophunzirawa akadzale mipingo padziko lonse lapansi ndikufikira anthu ochuluka omwe Yesu sadawafikire.

G. vesi 13-14 tikamupempha Mulungu zinthu zovomeredzeka mudzina la Yesu Iye adzatipatsa.

H. Yohane 14:15 akutipatsa ife malangizo amomwe tingakondere Yesu. Timamukonda Iye pamene timunvera muzonse. Ndichiphunzitso chachikulu chokhudzana ndikufunika koonetsa chikondi kwa Mulungu pomunvera Iye muchipangano chatsopano.

I. Yesu akulonjedza za munthu wachitatu mu Utatu wa Mulungu amene ali Mulungu Mzimu Woyera. Vesi 16-17 akulongosola za tanthauzo la ichi kwa okhulupirira.

i. tikuona apa kuti cholinga cha Mzimuyi ndikutithandidza ife. Machitidwe A Atumwi 1:8 akunena kuti Mzimu Woyera umatipatsa ife mphamvu. Mayendedwe athu muchikhristu,

amatheka chifukwa cha mphamvu ya Mzimu Woyera. Iyi ndi mphamvu yomwe imatipasa ife kulimbika, pa kulalikira ndi pakudzuzidwa.

ii. Vesi 16 ikunena kuti pamene Mzimuyi wabwera kwa ife, tsadzatisiyanso.

iii. Izi zikutanthaudza kuti pamene tapulumutsidwa, Mzimu Woyera amadza mwa ife (1 Akor. 6:19) pokhala kuti sadzatilekanso, timakhala otetedzeka muchipulumutso chathu. Tiyenera ngati akhristu kukhala omatsuka pozindikira kuti palibe chidzatilepheretse kukalowa Ufumu wa Kumwamba. Onani Aroma 8:35-39.

J. Vesi 20 ikutiphunzitsa ife za ubale wa Mulungu ndi mpingo wake.

K. Vesi 21-24 kachiwiri akulimbikitsa maganizo okonda Mulungu pakumvera Iye.

20. Mutu 15:1-17 Yesu akulongotsola kuti tsopano pali ubale watsopano pakati pa Iye, ophunzira ake ndi akhristu onse. Tonse ndife amodzi. Yesu ndi mpesa ndipo ife ndinthambi zake.

A. izi zikutiudza kuti akhristu onse akhale okangalika kutumikira Mulungu. Ndipo kuti tapatsidwa mphamvu yakuchita motere chifukwa cha m'gwirizano wathu ndi Yesu. Ndife amwayi kukwanitsa kutumikira Mulungu, koma ngati tilephera kutumikira Iye, tilibenso mwayi otumikira Iye. Sangatifunse kuti titumikire pamene nthawi zonse timanena kuti "ayi" akatifunsa kutero.

B. Vesi 9-13 tkuona zachikondi chopambana kwa ife kuchokera kwa Mulungu. Ndipo kachiwiri tikuonanso za kulumikizana kwakunvera kwathu ndi chikondi chathu pa Mulungu.

C. Vesi 12-13 tikuudzidwa za kuzama kwa chikondi cha Mulungu. Ndichikondi champhamvu, choti chidampangitsa Yesu kufa pantanda mosanyinyirika. Tikuona ganizo ili mbuku la Aroma 5:7-8.

D. Vesi 14-15 Yesu akutiudza kuti tili pa ubale watsopano ndi Iye. Amatitenga ife ngati abwenzi ake. Ndiulemu wanji wotere. Ndi ifenso ogwira ntchito limodzi ndi Yesu mu ufumu wake. Onani 1 Akor. 3:9.

E. Vesi 16 Yesu adatisankha Ife kukhala abwenzi ake ndi ogwira naye ntchito. Ndife ogwira ntchito limodzi ndi Yesu.

F. machaputala akusogoloku, Yesu akuphunzitsa kuti tiyembekedzere kuzunzidwa monga Iye adachitiridwa. Tikuwerenga apa kuti udani umenewu ukuchitika popanda chifukwa. Koma tiyembekedzere msautso. Mavesi 18-19 akuti monga dziko lapansi linada Yesu koteronso iwo akumutsata Iye lidzawada.

21. Chaputala 16:1-4 tikuudzidwa chifukwa chomwe tiyenera kuyembekedzera msautso, ndipo kutsausidwaku ndinjira yotikonzekeretsa Ife, koma ndi chithandidzo cha Mulungu, sitidzagonjetsedwa.

Zidzakhala choncho kuti tidzaima nganganga muchikhulupiriro. Muli zambiri muchipangano chatsopano zomwe zimatikonzekeretsa Ife kumsautso. Pakali pano pali akhristu ambiri amene akudzunzidwa kaamba ka chikhulupiriro chao.

A. Chaputala cha 16:5-8 ikutiphunzitsa za Mzimu Woyera.

B. Yesu akuti akuchoka pakati pao koma m’malo mwake padzabwera wina ndiye Mulungu Mzimu Woyera.

C. Mulungu Mzimu Woyera adzatitsutsa za machimo athu ndikutipanga Ife kukhala a khristu.

D. Yesu akuphunzitsa apa kuti ophunzirawa adzadandaula chifukwa chakuchoka kwake. Koma chisonichi chidzasandulika chimwemwe, chifukwa adzanvetsetsa kuti Iye adzagonjetsa dziko lapansi.

22. Mutu 17 pali pephero lopambana lokhudzana ndi mpingo. Pempherori limatchedwa pemphero la Mkulu Wansembe. Yesu ndi Wansembe Wankulu ndipo apa akupempherera akhristu okha.

A. Ili ndi pemphero lenileni la Ambuye. Lomwe timati pemphero la Ambuye limapedzeka mu Luka 11:1-4 ndipo limatiphunzitsa m’mene tingapempherere. Ili ndipemphero lenileni la Yesu limene anapempherera ife.

B. Choyamba kupempha vesi 1-5 ndiko kubwedzeretsedwa muulemerelo wake umene adautsiya asanabwere padziko lapansi kudzakhala munthu. Yesu adatsiya wina mwa ulemerero wake pamene amabwera padziko lapansi.

C. Kuchiyambi cha vesi 6 Yesu akupempherera akhristu onse. Muvesi 9 ndi 20 anati kuti pempheroli linali la anthu ake, osati osapulumutsidwa adziko lapansi. Ife akhristu ndife amtengo wapatali pamaso pa Mulungu.

D. Vesi 11ndi 15 Yesu akupemphera kwa Mulungu kuti atitsunge ife m’chikhulupiriro pamayetsero omwe timakumana nawo. Onani vesi 15 Yesu sadapempherere kuti okhulupirira achoke padziko lapansi ayi, koma kuwapulumutsa ku mazunzo. Akupempha Mulungu kuti atisunge ife m’chikhulupiriro ndikutitedza ife kuupandu wa oyipayo. Ndawerengapo za akhristu ena amene amapemphera pemphero limodzi uku akuzunzidwa. Samapempha Mulungu kuti awachotse m’mazunzowa, koma kuti cholinga cha Mulungu munsausowu chikwaniritsidwe komanso kuti akhalebe okhulupirika pamaso pa Mulungu.

E. Yesu akupemphera muvesi ya 17 kuti tikhale oyera ndipo mu vesi 22 kuti tikhale olumikidzana monga thupi limodzi. Ndiponso akupempha kuti tidzakhale ndi Iye (vesi 24)

F. vesi 14-16 tikuudzidwa kuti dziko lidzatida ife chifukwa sitili adziko lapansi. Dziko lapansi likulamulidwa ndi Satana ndipo kwathu kwenikweni ndi Kumwamba. Banja lanu lotsapulumusidwa limaganidza kuti ndinu opanda nzeru chifukwa cha khalidwe lanu ngati mkhristu. Komabe sangathe kukunvetsetsani.

23. Mutu 18:1-11 tikunvapo nkhani ya kumangidwa kwa Yesu imene ikuchitika m’munda wa Gesemani monga anenera Marko muuthenga wache wabwino. Yesu akudzipereka yekha kuti Yudasi atsavutike kumudzindikira. Tiyenera kunvetsetsa ndi kuyamikira kuti Yesu sadakakamidzidwe kuti akafe pamtanda. Adachita ichi chifukwa chachikondi chake kwa inu ndi ine.

A. vesi 12-27 tikunva zamulandu wa Yesu mbwalo la amsembe. Ndipo adamutengera Yesu kubwalo lamilandu la Aroma.

B. inali nthawi iyi yakuzengedwa kwa Yesu pamene Petro adakana Yesu katatu. Vesi 25-27 ikutiudza zakulira kwa tambala pamene Petro anamalidza kukana Yesu. Izi zikukwaniritsa chimene Yesu adachilotsera muchaputala cha 13. Pali phunziro lofunukira pamenepa kwaife

pamene Mulungu adamudzutsa Petro wogonjayu nampanga kukhala m'modzi wa akulu ampingo.

C. Akulu a Ayuda adafuna kumupha Yesu koma analibe ulamuliro wakuchita izi; choncho adamutumidza Iye kwa kazembe wa Aroma amene anali ndimphamvu za kupha Yesu.

D. Pilato anaziwa kuti Yesu anali opanda chifukwa, onani Yohane 18:38 ndi chaputala 19:4-6. Adayetsera kumatsula Yesu (onani vesi 12) koma Ayuda anatsutsana ndi zimenezi. Pilato amene amaopa Ayuda analamulira Yesu kuti apachikidwe ngakhale amaona kuti Yesu ndiotsalakwa.

24. chaputala 19 chikunena za kupachikidwa ndi kuikidwa m'manda kwa Yesu. Tikuona kuti maulosi amuChipangano cha Kale akukwaniritsidwa mukupachikidwa kwa Yesu. Ngakhale kupachikidwa kwa Yesu kunalotseredwa muChipangano Chakale, yense adachita chimenechi kwaiye kukuwerengedwa kuti wachita tchimo lopachika Yesu.

A. Masalmo 22:18 akukwaniritsidwa mu Yohane 19-24.

B. Eksodo 12:46 palibe fupa lomwe lidzathyoledwe, onani vesi 33ndi 36 muchaputala cha 19.

C. Zakariya 12:10 akukwaniritsidwa muchaputala 19:37.

D. Yesu anazunzika koopsa pantanda, kuthupi ngakhale kumalingaliro ake. Kupachikidwa ndiimfa yowawa zedi kwa munthu- ndinkhaza yoopsa zedi. Ndinthawi yokhayi kuchokera kale pamene Atate anatchera Mbuyo Yesu. Onani Masalmo 22:1-22 kuti munvetsese za m'mene Yesu anazunzikira, kuzunzikira ife.

E. Vesi 30 ndi 33 ikunena za imfa ya Yesu. Ndikofunika kuti tionepo bwino apa chifukwa adani ampingo akhala akunena kuti Yesu sanafe, koma kuti adangovulazidwa ndipo adachira. Tizindikire kuti palibe chifukwa chokayikira kuti Yesu anafa ndithu.

i. panali pantanda pamene Yesu adapambana nkhondo ndi Satana

ii. panali pantanda pamene Yesu adalipira tchimo lomwe linalipo, lilipo, ndi limene lidzachitidwe ndi mkhristu amene adakhalako ndi amene adzakhaleko.

iii. Satana akumenyabe koma wagonjetsedwa. Ntanda ndiofunikira kwa ife tonse.

25. chaputala 20:1-10 chikunena kuti kumanda kunalibe Mtembo wa Yesu. Ophunzira ake, sanazindikire kuti Yesu anati adzadzuka kwa akufa. Ngakhale ichi chinalotseledwa zaka za m'mbuyo zapitazo mu Masalmo 16:10 komanso pakuyamba kwa utumiki wa Yesu adanenanso za ichi m'malo ambiri monga Luka 24:46.

A. Machaputala otsalawa akunena za Yesu akuonekera kwa anthu otsiyanatsiyana. Ndizosangalatsa kudziwa kuti monga vesi 14 inena, Yesu koyamba adaonekera kwa mzimayi. Zoona zake monga zinenedwa mu Luka 24 Yesu adaonekera kwa azimayi ambirimbiri.

26. Chaputala 21:1-14 ikunena za Yesu akuonekera kwa ophunzira ake.

A. vesi 15-19 ikunena za utumiki wa Yesu kwa Petro pofuna kumubwezeretsanso. Petro anaziona kutsika kwambiri pamene adakana Yesu. Timawerenga za m'mene Yesu adatengera Petro ndikumubwedzeretsa kuutumiki. Phunziro ndilakuti palibe kanthu kuti mukunva kulephera kotani m'moyo mwanu, Yesu angakubwedzeretseni kuutumiki wa Ufumu wake. Petro anakhala m'modzi wa atsogoleri a mpingo amphavu kwambiri.

B. Yesu muvesi 18-19 tikunva za momwe Petro adzamwalirire. Mbiri imanveka kuti Petro adafa pa imfa yopachikidwa.

i. Mavesiwanso akunena za kuchuluka kwa anthu okalamba omwe ali ndi moyo. Okalambawa amalema nthupi mwao kuti achite Kanthu. Kotero pamafunika chisamaliro cha anthu omwe ndi a mphamvu. Kotero anthu okalamba amafunikira chisamaliro chofana ndi momwe anali ana.

C. Yohane akutseka buku lake ponena kuti Yesu anachita zinthu zambiri zomwe sizikanatheka kuzilemba zonsezi m'mabuku chifukwa bukulu likanakhala lalikulu lolephereka kunyamulidwa. Pamene tikumalidza kuphunzira mabuku a Uthenga wa Bwino pakufunikira kutsindika pa mfundo yakuti Yesu anafa ndithu komanso kumapeto patatha matsiku atatu anauka kwa akufa.

Imfa yake yapantanda ndipamene adalandira chilango chifukwa cha machimo athu, ndiponso kuti chinali chilango chimenechi chimene chatipatsa ife mwayi okalowa Kumwamba. Apa ndipomwe Satana analudza nkhondo.

Umboni wake ndi kuuka kwake kwa akufa. Adani ampingo akhala akufalitsa bodza limene lingapundule chkhulupiriro cha mpingo. Tikayang'ana mumbiri pali maganizo amene aperekedwa mumpingo amene amasimikidzira, m'mawu opepuka, za choonadi cha Baibulo. Chimodzi mwa mfundo zimenezi ndi Chikhulupiriro cha Atumwi. Tiyeni mwachidule tione chikhulupirirochi.

> Ndikhulupirira Mulungu Atate wa mphanvu zonse, wakulenga kumwamba ndidziko lapansi.
>
> Ndikhulupirira Yesu Khristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu, Amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa ndi Mariya namwaliyo,
>
> Nasautsidwa kwa Pontio Pilato; nafa, naikidwa m'manda,natsikira kwa akufa;
>
> Tsiku lachitatu nauka kwa akufa
>
> Nakwera kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wa mphanvu zonse,
>
> Kudzera komweko adzadza kudzawerudza anthu amoyo ndi akufa.
>
> Ndikhulupirira Mzimu Woyera,
>
> Ndikhulupirira Mpingo wopatulika wa Khristu wa kwa anthu onse, chiyanjano cha oyera mtima.
>
> Kukhululukidwa kwa machimo,
>
> Kuukanso kwa thupi
>
> Ndi moyo wosatha. AMENI.

## MACHITIDWE A ATUMWI

Bukuli limakamba za Yesu pamene amaonekera kwa anthu kotsilidza padziko lapansi ndi kukwera kwake kupita kumwamba. Limanena za kukhadzikitsidwa kwa mpingo ndikufalikira

kwake m’madera ena. Mpingowu unafalikira m’madera ena mwachangu chifukwa chamitsewu yabwino ndi chiyankhulo chodziwika ndi chotchuka muufumu wa chiRoma. Bukuli ndilotsavuta kuliwerenga komanso lodzala ndi zochitika zotsiyanasiyana. Muli malangidzo kwa ife a momwe tingapembedzere Mulungu ndi m’mene tingapangire zinthu zokhudzana ndi mpingo. Mpingo woyamba unakhadzikitsidwa ndi Atumwi, ndipo tingaphunzire zambiri pakuona zomwe amachita.

Timaphunzira zokhudzana ndi udindo wa akulu ampingo komanso atumiki mumpingo, ndi zomwe ayenera kuchita mumpingo. Timaphunzira zambiri zokhudzana ndi Mulungu komanso Mzimu Woyera amene ali nthandidzi wathu wankulu komanso ntetedzi ndi mphuzitsi. Chimodzimodzi ndi ife lero, mpingo umenewu unakumana ndi mikwingwirima yambiri. Pachiyambi amene amawadzunza anali Ayuda. Aroma adadzindikira kuti chikhristu chinalidi chipembedzo cha uzimu ndipo sichinali chiopsezo ku boma la Aromawa. Panapita zaka makumi atatu pamene Aroma anayamba kutsautsa mpingo wa akhristu.

Chipembedzo cha Chiyuda chinavuta kwambiri kunja ngakhale nkati mwa mpingo wa chikhristu. Timawerenga mbukuli zamomwe mtumwi Paulo anadzudzira mpingowu asanakhale mkhristu iye mwini. Ayuda omwe analowa muchikhristu anafunitsitsa kuphatikidza zomwe amakhulupirira ngati Ayuda ndi kukakamidza ena kuti adzipanganso chimodzimodzi. Tiona nkhondo yomwe inamenyedwa pokhadzikitsa mfundo yakuti chikhristu chinali chotsiyana ndidzikhulupiriro zina ndipo chinali chopanda msankho ndipo kuti amitundu adali olandiridwa muchipembedzo chimenechi, ndipo sanalinso otsalira monga Ayuda amaganidzira. Zina mwa zinthu zofunikira m’bukuli ndi zozizwitsa zomwe zalembedwanso momwemu. Pamodzi muli zozizwitsa zokwana 25 mubuku limeneli. Zayambira pa kuuka kwa akufa kukafika pamene zitseko za m’ndende zinatseguka, komanso pamene Paulo analumidwa ndi njoka yomwe sinamuvuraze. Ndipo zozizwitsa zimenezi zinathandidzira mpingo womwe unali wakhanda kukhadzikika kopotsa. Zozizwitsa zimenedzi zinachitira umboni ku choonadi cha Uthenga Wabwino umene anthu amaulandira.

Chaputala 1:1-11 tikunvamo za matsiku omalidza aYesu padziko lapansi ndiulendo wake opita kumwamba. Anatha matsiku okwana 40 atsanakwere kumwamba. Ndipo amaonedwa ndi anthu otsiyanatsiyana. Vesi 1-2 ikutiudza kuti nthawi imeneyi Yesu anali kuphunzitsa ndi kulamulira mpaka kufikira tsiku lomwe anakwera kumwamba.

1.Vesi 8 tikuonapo zamau otsilidza komanso otchuka omwe Yesu adanena atangotsala pang’ono kuti akwere kumwamba. Timadziwa kuti munthu amayankhula zinthu zofunikira pamene wadziwa kuti ndikotsilidza kwa iye  kuyankhula kugulu la anthu. Yesu kachiwiri akutilamula ife kukaudza ena za iye kudziko lonse lapansi. Chinthu chachiwiri chomwe ndichofunikira kwambiri kumpingo pambuyo pa kupembedza ndi kufalitsa uthenga wa Mulungu. Vesi 8 ndiyabwino kwambiri kuti tiilowedze. Ikutilimbikitsa ife kulalikira m’mudzi wakwathu ndi ina yodzungulira komanso kumalekedzero adziko lapansi.

A. Atumwi ndi mpingo woyambawo adasunga malangidzowa pansi pa mtima wawo. Mwachangu adafalitsa uthenga wabwino muufumu wonse wachiRoma komanso kupitirira kumeneko. Komabe chidwi chofalitsa uthenga padziko lonse lapansi panopa chachepa zedi ndichifukwa chake chikhristu chayamba kubwerera m’mbuyo m’madera apadzikoli. Akhristu ambiri saudza ena za Yesu kuti ndindani chimene chili chinthu cholakwka kwambiri.

2. vesi 9-11 akufotokoza za momwe Yesu anakwerera kumwamba. Pamene adalowa m’mitambo. Vesi 11ikutiudza ife kuti adzabweranso chimodzimodzi. Tikudziwa kuti Yesu adzabweranso, koma sitidziwa nthawi yache, ndipo aliyense amene adzayetsere kunenera za nthawi ya kubwera kwake mutengeni kukhala onama.

3. mavesi enawo muchaputalachi akufotokodzera zomwe zimkachitika pamene amadikira kubwera kwa Mzimu Woyera. Tikuona mu vesi 14 kuti nthawi ina yonseyo anali mkupemphera ngati gulu. Mpingo ukuyenera kupemphera mogwiridzana/pamodzi.

A. Muvesi 15 tikuona Petro akutenga udindo otsogolera mpingo. Anali Petro osinthika kumalekedzero kwa utumiki wa Yesu pano padziko lapansi.

B. Vesi 26 ikutiudza za kutsankhidwa kwa Matiyasi kulowa m'malo mwa Yudasi. Sitimadziwa zambiri za iye kupatula kuti anali olowa m'malo mwa Yudasi.

C. Atumwi adali amuna amene adatumidwa ndi ulamuliro wapadera wa Yesu Khristu. Mwachitsanzo Aroma 11:13 imati Paulo anali mtumwi wa kwa amitundu. Tikati Atumwi mu Baibulo timatanthaudza otsatira a Yesu amene anamuona iye maso ndi maso. 1 Akor. 9:6

F. ophunzira ndi otsatira a Yesu ndipo a khristu tonse ndi ife ophunzira a Yesu. Kukumana pamodzi ndi kupemphera ndi magawo ofunikira kwambiri m'moyo wa chikhristu. Izi zimatchulidwatchulidwa m'Baibulo. Mwachitsanzo Mac. 2:46-47, Mac. 4:23-24, Mac.5:12 Mac15:25, Aroma15:6 Aefeso 5:18

Muchaputala 2:1-13 tikuonapo za kubwera kwa Mzimu Woyera, komwe ndichinthu chofunika kwambiri. Izi zinachitika patatha matsiku 50 chidzukire Yesu Khristu tsiku loyamba la sabata.

1.Vesi 1-3 ikufotokodzera zamomwe Mzimu anatsikira.

2. Vesi 4-18 akunena za momwe akhristu anadzadzidwira ndi Mzimu Woyera, ndipo anayankhula kwa anthu, aliyense mchilankhulo cha kwawo, ndipo onverawa amamva bwinobwino zonenedwa zonsezi zomwe akhristuwa amafotokodzera m'mene amagawa Uthenga wabwino. Izi zimatchedwa kuyankhula m'malilime. Dziwani kuti cholinga cha malilime kunali kufotokodzera Uthenga Wabwino kuti aliyense ndinjira imeneyi amve kutsiyana ndikuyankhula chiyankhulo cha mtundu umodzi wa anthu. Onani 1Akor. 14:26-28 kuti muone malangizo ena okhudzana ndi kuyankhula m'malilime.

A. Mac. 10:46 akulungotsolanso za ntchito ya malilime komwe ndiko kulumikidzana ndi Mulungu. Ntchito yoyamba ya malilime m'Baibulo ndiko kuyetsera kufalitsa choonadi chokhudzana ndi Mulungu.

3. Petro muchaputala cha 2:14-36 akulalikira Uthenga wamphamvu kwambiri.

A. adanena za nthawi akukhalamo kuti ndi nthawi ya kukwaniritsidwa kwa maulosi am'mbuyomu. Adayankhulanso kwambiri za nthawi yotsiyanatsiyana ya maulosiwa imene inakwaniritsidwa ndi kubwera kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

i. choyamba kunena chinali chakuti anthuwa sanali oredzera monga ena amaganidzira. Kusanulilidwa kwa Mzimu Woyera kunalotseredwa mu buku la Yoweri 2:1-32

ii. kumayambiriro kwa Mac. 1:16 ndi 20 kuperekedwa kwa Yesu ndi Yudasi kunalotseredwa Muchipangano Chakale, onani Masalmo 41:9

iii. Mumachidwe 3:18 Petro adawalongotsolera momwe kunalembedwera za momwe Yesu adzanzunzikire (Masalmo 22 ndi Yesaya 53).

iv. Mac. 2:23-28 Petro akuyankhula kuti kuuka kwa akufa kwa Yesu kunanenedwa mu Masalmo 16:10 pamene amati Yesu sazaona chivundi, zomwe ndidzotsiyana ndi munthu

yemwe ali m’manda amene amaola ndithu. Koma ndi Yesu zinali chomwechi chifukwa sadakhalitsemo m’mandamo.

v. Mac. 2:33-35 tikunva kuti kukwera kumwamba kwa Yesu kunalotseredwa mu Masalmo 110:1.

4. Mac. 2:41 tikuonamo za momwe anthu analandilira uthenga wa Petro pamene anthu 3000 adatembenuka mtima malo omwewo kukhala akhristu.

5. Vesi 42-47 ikulongotsola umodzi wa iwo amuchikhulupiliro. Tikuona kuti iwo anali odzikhuthula ku ntchito yophunzitsa ndi kukhala mu umodzi chomwe ndichitsanzo chabwino kwa ife. Timaphunzira kuchokera mu vesi 47 kuti Mulungu ndiyemwe amachulukitsa anthu mumpingo.

Chaputala 3:6 tikuona kuti Petro ndi Yohane apatsidwa mphamvu zopereka machiritso. Vesiyi ikunena kuti mphanvu zimenezi zinachokera kwa Yesu. Dziwani kuti samalipiritsa chinachilichonse akachidza munthu. Vesi 11-26 akupereka chifukwa chomwe chapangitsa kuti akhale ndi mphanvu zimenezi komanso chomwe chapangitsa kuti achidze munthuyu. Ichi chidapanga anthu kubwera kwa Yesu.

Chaputala cha 4:1-4 tikunva zoti akulu a chipembedzo cha Ayuda anazungudzika chifukwa adaona kuti zochita Petro ndi Yohane zimapangitsa anthu kukhulupirira Yesu kotero adawamanga iwo. Ndichifukwa ninji panali upo otere?

1.timawerenga mu vesi 4 kuti anthu pafupifupi 5000 adatembenuka ntima kuyenjedzera 3000 amene anatembenuka mtima patsiku la pentekosite lija. Aulamulowo adawaopsetsa ndikuwachenjedza atumwiwo kuti asaphunzitse ndikuyankhula chilichonse chokhudzana ndi Yesu. Muvesi 19-20 Petro ndi Yohane ananenetsa kuti adzapitiridza kuyankhula choona. Ifenso akhristu lero tiyenera kukhalan ndi mtima uwu wamphanvu poudza anthu zokhudzana ndi Yesu ngakhale kutakhala kuti izi zitha kubweretsa chiopsezo pa moyo wathu.

Chaputala 5:1-11 tikunva za nkhani yotchuka kwambiri yokhudzana ndi Hananiya komanso Safira mkazi wake. Nkhani iyi idachitika pamene anthu amagulitsa minda yao ndikupereka ndalamazo kumpingo kuti zithanidzire pa kutumikira Ambuye. Hananiya ndi mkazi wake analonjedza kuchita chomwechi, koma atagulitsa munda wawo anatenga ndalama zina nadzitsunga. Sikuti anali okakamizidwa kupereka ndalama zonse kumpingo ayi. Koma chifukwa adalonjedza kwa Mulungu kuti adzapereka ndalama zonse, pamenepa mwini ndalamazo anali Mulungu chifukwa chalonjezolo. Ndipo chilango chakubachi inali imfa. Tiyenera kutsamala kutsunga malonjedzano athu kwa Mulungu. Mukuganidza kuti ndichifukwa ninji Hananiya adalonjeza ndalama zonse kwa Mulungu pamene amadziwa kuti sapereka zonse? Kapena mwina amafuna kudzionetsera kuti iye ndioolowa manja? Tiyenera tidziyetsetsa m’mene tingathere kusunga zonse zimene tinalonjedza kuti tidzachita kwa Mulungu. Ngati talephera kutsunga lonjedzo chifukwa tinatsowa mphamvu zotsungiradzo, Mulungu adzatikhululukira tchimolo. Mulungu amadziwa mitima yathu ndipo adzatitsungira mulandu pamene tasankha kutsasunga malonjedzo athu pamaso pake.

Chaputala cha 5 chimanena za kumangidwa kwa atumwi, ndipo vesi 18-20 timanva momwe mngelo wa Mulungu anawatulutsira mndende, ndikuwalamula kuti apite kukachitsa ndikuphunzitsa uthenga wabwino. Apanso kachiwiri atumwi adapititsidwa kubwalo la milandu la Ayuda. Vesi 28-29 timaonapo chiphunzitso chofunikira kwambiri. Sitiyenera kunvera Malamulo a dziko ngati ali kutsutsana ndi Mau a Mulungu. Ngati titero ndiye kuti tikunvera munthu otsati Mulungu. Tikuyenera kuchita motero ngakhale kuti ichi chingatsiye

moyo wathu pa chiswe. Tikuona vesi 40 kuti adakwapula atumwiwo. Dziwani khalidwe la atumwiwo mu vesi 41ndipo kuti adapitiriza monga vesi 42 inena kuphunzitsa ndikunena zambiri zokhudzana ndi Yesu. Antchito a khristuwa sadalolere chilichonse kuletsetsa ntchito ya Mulungu yomwe adayiyamba kuti ilekedze panjira.

Chaputala cha 6:17 tikuona gwero la udindo wa atumiki/madikoni. Chaputala cha 6 timanva kuti amuna 7 anasankhidwa kuti agwire ntchito yotsamalira amatsiye kotero kuti atumwi (akulu a mpingo) adzangokhadzikika kulalika ndikuphunzitsa Mau a Mulungu. Tikuona kuti udindo wa atumiki udakhadzikitsidwa ndi Mulungu.

A.Vesi 7 tikunva zotsatira za kuphunzitsa ndi kulalikira Mau aMulungu ndi akulu a mpingo kuti kunali kuchuluka kwa chiwerengero cha anthu mumpingo.

Chaputala 6:9-60 tikunva zamomwe Sitefano mtumiki woyamba adafera chifukwa chachikhristu.

1. chaputala 6:9-7:1 Sitefano akugwiridwa ndikupititsidwa kubwalo lamilandu la Ayuda.

A. chaputala 6:12-14 tikunva za momwe anthuwo ananamira napereka umboni wonama wotsutsa Sitefano.

B. vesi 10 ndi 15 tikunvapo kuti Sitefano analimbikitsidwa ndi Mzimu Woyera, ndikutinso anatsunga mtendere pamene amakumana ndi adani ake.

C. Chaputala cha 7:1 tikunva Sitefano akufunsidwa ngati mulanduwo unali woona. Adayamba, pa vesi 2 kuyankhula ndime yaitali kufotokodzera Mbiri ya Ayuda kuchokera pa Abrahamu mpaka kufikira pamene kachisi anamangidwa.

2. mavesi a 51-53 Sitefano akunena zotsutsana ndi akulu a Ayuda zimene zinapanga iwo kukwiya ndi iye. Ndipo adamuponya miyala nafa iye.

A. kodi Stefano adapedza kuti chilimbikitso? Vesi 55 ikuti ichi chinachokera kwa Mulungu Mzimu Woyera. Phunziro kwa ife ndilakuti tikhale okonzekera kufa ngati ndikofunikira kutero chifukwa cha Ufumu wa Mulungu. Koma tiyang'ane kwa Mulungu kuti atipatse mzeru yochita monga Sitefano anachitira ndi kulimbika komwe akutionetsera. Mpingo wa akhristu unamangidwa ndi mwazi wa ophedwa chifukwa cha Yesu. Mac.12:2, Mat. 14:10.

B. onani vesi 58 ndikuona kuti nsogoleri wa chikristu anali m'modzi wa anthu omwe amagenda miyala Sitefano. Kodi anali yani?

CHAPTALA 8 NDI 9 NDIMITU YOKHUDZANA NDI SAULI-PAULO

1.Chaputala 8:1-3 tikuona kuti Sauli akuchilimika pomapha akhristu.

2. kenako tikuwerenga mu chaputala cha 9:3-8 Paulo akuona chimene chimatchedwa kuti choona Paulo panjira ya ku Damasiko. Pamene adakumana ndi Ambuye ndipo anatembenuka mtima. Onani Vesi 15 pamene akuti Paulo adasankhidwa ndi Iye kuti afalitse uthenga wabwino. Ndipo mu vesi 16 ikulotsera kuti Paulo adzadzunzika potumikira Ambuye ndipo Mbiri imati Paulo adazunzika ndithu.

3. Machitidwe 9:20 Paulo adayamba kulalikira zokhudzana ndi Yesu. Kawirikawiri amakhala ndi chidwi chofalitsa uthenga okhudzana ndi Yesu. Koma pakapita nthawi yochepa amalema naleka. Koma titenge chitsanzo cha Paulo amene sadalekedze m'moyo mwake kulalikira mpaka kufikira kumapeto kwa moyo wake, pamene adali kupereka uthenga wa momwe anthu

angapulumutsidwire. Tikhale okonzeka kulalikira uthenga wa Yesu ndi kufikira anthu ndi uthenga umenewu.

Chaputala 9:36-chaputala 12

1.chaputala 9:36-42 Petro aukitsa mzimayi otchedwa Dorika. Mavesiwa amanena kuti ambiri adalowa chikhristu chifukwa cha chinthu chimenechi.

2. timawerenga muvesi 14 kuti dzina lina la akhristu ndi Oyera mtima. Akhristu onse ndi oyera mtima. Otsati ochepa amene anthu ena anawayeneredza.

3. chaputala cha 10-11:18 timaphunirapo zinthu ziwiri zofunikira kwambiri.

A. tkuona pa 10:9-16 komanso 11:5-10 kuti Malamulo achikhalidwe okhudzana ndizakudwa zodetsedwa ndi zotsadetsedwa atha ndikubwera kwa Yesu khristu. Yesu adaphunzitsa ichi mubuku la Marko 7:14-19 pamene amalongotsola kuti cholowa mwa munthu sichiipitsa munthu koma ndichotuluka mwaiye chimene chimamuyipitsa kapena kumukonza. Ndimtima umene umatulutsa maganizo ndi zintchito zoipa kunja kwa munthu.

B. izi zidachitika chomwechi pokonzekeretsa Petro ndi abale onse kulandila amitundu mu mpingo. Petro tsono akulalikira uthenga wachipulumutso wa Yesu kunyumba ya Korneliyo. Ndipo Korneliyo ndi anzake anapulumutsidwa. Chaputala 10:44 akuti Mzimu Woyera unatsikira kwa anthuwa.

C. muchaputala cha 11:2-3 Petro akudzudzulidwa ndi Ayuda achikhristu amene samanvetsetsa kuti Yesu ndi wa kwa anthu onse. Vuto lalikulu mu mpingo woyamba linali lakuti akhristu ambiri Achiyuda, samafuna kuti amitundu alowenso chikhristu. Ndiponso amaona kuti amitundu azichita zonse za chipembezo cha Ayuda monga mdulidwe kuti aloledwe kukhala akhristu. Petro adayankha msutso umenewu poudza anthuwo za chimene Mulungu adamuyankhula iye. Vesi 18 ya chaputala cha 11 ikunena kuti akuyenera kunvetsetsa Mulungu wapereka mphaso ya kulapa kwa anthu onse. Mulungu amakonda anthu ake onse mofanana. Sakondera mtundu umodzi wa anthu kapene akhristu akale kutsiyana ndi atsopano.

3. chaputala 11:26 tikunva kuti kunali ku Antiokeya kumene kumene okhulupirirawo anatchedwa akhristu.

4. chaputala cha 12 chikuthirila ndemanga za nsautso yayikulu ya Akhristu kuchokera kwa Ayuda zomwe zidapangitsa akhristu ambiri kuthawira kumadera otsiyanatsiyana adziko lapansi.Ichi chinali chifukwa chomwe chidapangitsa kuti chikristu chifalikire kudziko lapansi pamene akhristu othawawo anali kufalitsa uthenga wa Yesu kwa abale omwe amawapedza kumaiko omwe amathawirawa.

A. vesi ya 2 tikuphunzira kuti mtumwi Yakobo anadulidwa mutu ndi mfuma Herodi Agripa. Vesi 3 ikunena kuti Petro adatsekeredwa kundende. Tikuona kuti ndi zanja la Mulungu Petro adatuluka mundendeyi. Herodi amachita zonsezi pofuna kutsangalatsa Ayuda ngakhale amadziwa kuti kuzunza Petro ndi Yakobo chinali chinthu chotsayenera.

B. vesi 21-23 tikuona momwe Herodi anavomeredzera kuti atchedwe Mulungu ndichilango chomwe Mulungu adapereka kwa Herodi chifuwa cha kudzikudza kwake. Imfa yomwe adafa inali yowawa kwambiri.

Chaputala 13-14 ulendo woyamba wa Paulo ndi Banaba. Tikudziwa kuti Paulo adayenda maulendo atatu kukafalitsa mau a Mulungu.

1.Vesi 2 yachaputala cha 13 Mzimu Woyera unayitana Paulo ndi Banaba kuti apatulidwe kupita kukafalitsa uthenga wabwino. Vesi 3 pali malangidzo abwino kwa ife okhudzana ndi kufunikira kwa pemphero ndi kutsala kudya tisanayambe ntchito ya Mulungu. Tiyenera kunva kuitana kwa Mulungu tisanayambe kugwira ntchito yake. Njira imodzi yodziwira kuti ndi iwe oyitanidwa ndi Mulungu ndi kupemphera ndi kutsala kudya ndikufunsa Mulungu kuti akutsogolere. Dziwani kuti kutumidza anthu kukalalikira uthenga wa chipulumutso inali mbali imodzi ya mpingo woyamba. Tiyeneranso kuchita chomodzimodzi. Titha kutumidza okafalitsa uthenga kudera lakwathu komanso padziko lonse lapansi.

2. Ulendo woyamba wa mtumwiyu unali okafikira amitundu omwe amapedzeka ku Asiya komwe kukudziwika ndi dzina loti Terkey. Kunali chipambano pokhala kuti anthu adatembenuka mitima ndiponso kunali kulepherekanso kwa ntchito chifukwa kudali nsunso waukulu kwambiri. Ayuda adalimbana nawo kwambiri ndipo tikuwerenga muchaputala cha 14:19-20 kuti anamuponya iye miyala kutsala pang'ono kufa. Komabe, timawerenga kuti Paulo adadzuka napita kudera lina nakalalikira uthenga wa Mulungu. Paulo amakondadi Mulungu ndipo sanatsiye kulalikira ngakhale izi zimaika moyo wake pachiopsezo cha imfa. Kodi takonzekera kutumikira Mulungu ngakhale izi zingachititse kuti moyo wathu ukhale pachiopsezo cha imfa kapena tingotsata Mulungu ndicholinga chopedza phindu? Khalidwe la Paulo ndikhalidwe lomwe likufunikira kwa mkhristu woona mtima.

3. chaputala cha 14:23 mpingo woyamba unatsala kudya pamene umadzodza akulu ampingo. Tiyenera kuphunzira chinthu chimenechi ndikuchitanso chimodzimodzi.

Chaputala 15 chikukamba za kusagwiridzana mumpingo.

1. Ena mwa akhristu achiyuda adapitilidza kulimbikitsa kuti otembenuka amitundu akuyenera kulandira mdulidwe, izi sizoonayi. Paulo ndi Banaba ndi akulu ena ampingo adati mdulidwe sukuyenera chifukwa pakutero kudzakhala ngati chipulumutso chimalandiridwa chifukwa cha ntchito. Baibulo limaphunzitsa kuti timapulumuka chifukwa cha chifukwa cha chikhulupiriro ndpo kuti Yesu anagwira kale ntchito yonse.

2. akuluwa adagwiridzana kuti sikunali koyenera kuchita mdulidwe ndipo vesi 19-20 ikufotokoza kuti adatumidza makalata olengedza uthenga umenewu. Makalatawa anali kupempha akhristu achiyuda ndi amitundu kuti apewe zinthu zomwe zingamayambitse mapokoso pakati pao. Akhristu achiyuda adaletsedwa kukakamidza amitundu ku mdulidwe ndipo amitundu adaletsedwa kudya magazi. Ili linali ganidzo labwino chifukwa adamenyetsa nkhwangwa pamwala polimbikitsa mdulidwe, zinthu zimene sizofanana ndi chiphunzitso cha Baibulo. Koma amalephera kuwasutsa pa nkhani ya kudya mwazi poitenga kuti ndiyaing'ono ndikuyetsa kuti pakutero atha kukhumudwitsa anthu ena. Ifenso tisamale pochita zinthu zimene zikulimbikitsidwa ndi Baibulo.

A. chitsanzo kwa ife akhristu alero ndi nkangano wathu pankhani za m'mene ubatizo ungapangidwire. Akhristu ena amakhulupirira kuti ubatizo weniweni ndi womidza thupi lonse. Pamene ena amakhulupirira ubatizo ongotsanulira. Titsamataye nthawi potsutsana pa zinthu izi chifukwa munthu sazapulumutsidwa malinga ndi njira yomwe anabatidzidwira. Akhristu tikuyenera kugwirira ntchito limodzi.

3. tikuona muvesi 28 mfundo yofunikira kwambiri. Ndimalamulo okhawo amuBainulo amene akhristu ayenera kuwatsatira. Tidziletse poyenjedzera malamulo ngati Afalisi amachitira zomwe zinapangitsa Yesu kukhala onyatsidwa kwambiri. Chitsanzo paichi ndi pamene mpingo uletsa kuphika tsiku lasabata.

4. Vesi 36-41 tikunvapo za kutsemphana maganizo kwa Paulo ndi Banaba potenga Marko paulendo wao wachiwiri wokalalikira uthenga wabwino. Pamapeto azonse anthuwa analekana napita malo otsiyana, ndipo sitikunvaso kuti anthuwa analumikidzana nagwiranso limodzi ntchito. Zotsiyana ndizimene zimachitika mumipingo yathu matsiku ano, sitikuona apa kuti anthuwa adamenyana ayi. Ndizotheka kusemphana maganizo pazinthu za utumiki koma tipitirirebe kukhala abwenzi ndikugwirira ncthito limodzi. Panali zotsatira zabwino chifukwa chakulekana kwao pakuti aliyense adapita mbali yake nafalitsa uthenga wa Ambuye. Chaputala cha 16-20 chikunena za ulendo wachiwiri ndi wachitatu wa Paulo. Sitiwatotokodzera kwambiri maulendo amenewa kaamba kanthawi. Tingoona mfundo zochepa chabe. Ndikwabwino kuti muwerenge machaputala amenewa painu nokha.

1. Mac. 16:7 ndiphunziro lathu kwa ife kukhala ochilimika pa kutsogoreredwa ndi Mzimu Woyera. Mulungu ndiye mwini ulamuliro, ndipo tiyetsetse kudziwa chifuniro chake ndi kuchinvera.

2. Mac. 17:23 akunena za kuputsa kwa anthu popembeza Mulungu wotsadziwika m'malo mwa Mulungu woona ndi wamoyo amene wadziulula yekha M'malemba. Kwanthawi yaitali akhala akupita ndi kupembedza milungu yonama yomwe anaikonza m'malo mwa Mulungu woona. Malo ambiri zaka zino akunenetsa kuti kulibe Mulungu, m'malo mwake akutenga sayansi ngati mulungu wao. Akumbembedza mulungu wobodza amene wopanga ndi manja awo.amapembedza mulungu wotsadziwika monga vesi 23 inena.

3. Mac. 17:29-31 ikunena kuti Yesu atsanabwere Mulungu analeza mtima kopotsa. Pano tsopana zinsitsi zonse za chipulumutso zavumbulutsidwa ndipo anthu onse akuitaniridwa ku kulapa ndikukhulupirira pa Yesu. Paulo pamavesi atatuwa akupereka zifukwa zitatu zopangitsa anthu kuti alape machimo. Munthawi yachipangano chakale Ayuda adali kupuumutsidwa chifukwa cha Mesiya amene amayembekedzeredwa kudzayo. Ife lero timapulumutsidwa poyang'ana pantanda wa Yesu amene pano timamudziwa ndi dzina chabe.

A. Mulungu watiledzera mtima kwa nthawi yaitali. Koma nthawi idzafika ndipo Iye adzalimbana ndi onse amene sadalape.

B. Mulungu dwalamulira onse kulapa kuti apulumutsidwe. Mac. 2:38

C. Mulungu wasankha tsiku lotsilidza la zonse pamene Yesu adzakhale owerudza wake.

4. Chaputala cha 20:7 chikunena kuti akhristu oyamba amakumana tsiku loyamba la sabata lomwe ndilamulungu.

Chaputala 21-26 tikuona za kubwerera kwa Paulo ku Yerusalemu.

1.chaputala cha 21 tikuona za kumangidwa kwa Paulo chifukwa cha khama lake pa uthenga wabwino.

2. chaputala cha 23 tikuona Paulo akuimikidwa mu bwalo la Ayuda lomwe Yesu anawerudzidwamo mopanda chilungamo.

3. Ayuda adalimbana okhaokha kodetsa nkhawa kuti chipolowe chidayambika ndipo Aroma anadza namukwatulapo Paulo. Muchaputala cha 24:11 Mulungu akumutsimikidzira Paulo kuti zonsezi zikupangika ndicholinga chofuna kumutsegulila iye njira yopita ku Roma kuti akafalitse uthenga wabwino kumeneko.

4. vesi 12-14 tikunva kuti Ayuda adali okwiya kwambiri ndi Paulo ndipo 40 mwaiwo adachita chowinda choti asadye ndikumwa mpaka atapha Paulo. Mwina anafa posachedwa chifukwa

cha luzu komanso njala chifukwa Mulungu sadawalole iwo kupha Paulo. Paulo anali nzika wa chiRoma zomwe zimamupatsa chitetezo cha Malamulo kotero Paulo adatumizidwa kwa Felikisi kazembe amene adafunsa Paulo ndipo anamutumidza iye kundende kumene anakakhalako zaka ziwiri. Kazembe watsopano zina lake Festo adazenga mulandu Paulo pogwiritsa ntchito oweruza Achiyuda amene Paulo adawakana. Paulo adali ndi ufulu ngati nzika ya chiRoma kusankha kukawerudzidwa ndi ndi Kaisala zomwe Mac. 25:11 tikuudzidwa kuti izi ndizomwe adachita. Umu ndimomwe Mulungu adakonzera kutumidzaPaulo kuRoma monga Iye adakonzera.

6. kachiwiri tikuona mfumu Agripa akubwera kudzakumana ndi Paulo ndipo pamodzi adanfunfuza Paulo. Mac. 25:25 Festo akunenetsa kuti sadapedze choipa chilichonse mwa Paulo. chifukwa chomwe Festo sadamumatsule Paulo ndi chofana ndi chifukwa chimene chidapangitsa Yesu kutsamatsulidwanso pamene adapedzeka otsalakwa. Kunali kufuna kutsangalatsa Ayuda ngakhale kunali kulakwitsa kuchita zotere. Akazembe amenewa ndi Pilato adachita zinthu zofana pamene adakana kumatsula munthu amene adadziwa kale kuti alibe mulandu. Tiyenera nthawi zonse kuchita zinthu zomwe zimakomera Mulungu ndikusaganidzira zomwe munthu aganidze tikachita motere.

7. chaputala cha 26 chikunena momwe Paulo adadzitetedzera yekha ponena Mbiri yake ngati mfalisi, kutembenuka mtima kwake, ndim'mene adalalikira uthenga wabwino chomwe ndi chifukwa chidapangitsa Ayuda kumuukira Iye.

A. Paulo adalalikira uthenga wabwino kwa mfumu Agripa amene pa vesi 24 adati Paulo wapenga misala. Paulo adayetsera kuwaunikira amfumuwa kuti akhale mkhristu.

B. Vesi 27 Paulo akutsendera kuyetsa kwake popanga mfumu Agripa kukhala mkhristu. Taonani yankho loputsa lomwe mfumu Agripa akunena pa vesi 28 pamene aphiphiritsa zonenedwazo. Mulungu adalolera Agripa kuumitsa mtima wake ndikukana uthenga wopulumutsa moyo. Ndipo nthawi yochepa zitatha izi Agripa adamwalira ndipotu kunali kovuta ndiponso mochedwa kwa iye kulandira Mulungu amene Paulo adamulalikira.

8. Vesi 31-32 ikunena kuti ngakhale Festo kapena Agripa sadapedze chilichonse cholakwa kwa Paulo. Paulo akadamatsulidwa akanakhala kuti sadasume nkhaniyakeyi kubwala la Kaisala Mfumu yaikulu ya kuRoma. Iyi idali njira yomwe Mulungu adagwiritsa ntchito pomutumidza Paulo KuRoma kuchokera ku Yerusalemu.

Chaputala 27-28 Paulo apita ku Roma

1.Ulendo wa ku Roma udachitika panthawi yovuta, nthawi yanamondwe wa panyanja. Tikuwerenga kuti namondwe oopsayi adaswa chombo chomwe Paulo adakwera pa chisumbu cha Melita. Chombocho chidasweka modetsa nkhawa, koma Mulungu adapulumutsa moyo wa wina aliyense adali muchombocho monga Paulo adalotsera nthawi yoyamba ija pa Mac. 27:34.

2. Paulo adapedzeka pachisumbu chimenechi cha Melita atangotsala pang'ono kufika ku Itale. Mulungu adapitiridza kumutsamala iye ngakhale panthawi yomwe adalumidwa ndi njoka pamene sadanve ululu kapena vuto lililonse chifukwa cha ngoziyo. Phunziro pamenepa ndilakuti tiyenera kugwira ntchito ya Mulungu molimbika. Ngati Iye adatizunzikira, ndichachidziwikire kutinso adzatitetedza, ndipo pamapeto pazonse adzatitenga kupita nafe kumwamba.

3. Ndipo nyengo yachitsanu itatha Paulo adapitilidza ulendo opita ku Itale. Tikuona mu chaputala cha 28:14 kuti ngakhale ku Itale komweko panthawiyi chikhristu chinali chitayamba kale.

4. Tikuona kuti ngakhale Paulo adali omangidwa komabe amaloledwa kuphunzitsa alendo ake onse choonadi cha Yesu Khristu. Tidziwe kuti palibe chidzalepheretse ganidzo la Mulungu kuti litsachitike, Mulungu adafuna kuti Paulo apitilidze kuphunzitsa ngakhale kundende.

## AROMA

Iyi ndikalata yolembedwa ndi Paulo. Muli makalata okwanira 21 amene adalembedwa ndi cholinga cholangidza akhristu za chomwe angakhulupirire ndi m'mene angakhalire m'moyo wa chikhristu. Makalata ena adalembedwa ndicholinga chokonza zolakwika za mimpingo ndi zamunthu payekha. Pa makalata 21, Paulo adalemba makalata 13.

Buku la Aroma lidalembedwa kupita kumpingo wa  Aroma Paulo asadapite kumeneku. Ili ndibuku labwino kwambiri limene limaphunzitsa za ziphunzitso zikuluzikulu za muBaibulo. Tikuona kuti muthu wina aliyense ali ndi chifukwa ndi Mulungu ndipo akufunikira chipulumutso payekha. Paulo adaphunzitsa momwe munthu angalungamitsidwire, ndipo kuti tingakhale bwanji ngati akhristu. Bukuli likunenanso zazomwe Mulungu azachitire Ayuda. Paulo sakungonena za momwe tingakhalire moyenera ndi Mulungu, koma akupereka chitsanzo ndi kudzipereka kwake kwa Ambuye ndikupita chitsogolo potumikira Mulungu ngakhale munthawi ya nsauso yaikulu pa moyo wake. Ndibuku lodzala ndi zinthu zochitika. Titha kutha chaka tikuphunzira buku limeneli koma otsamalidza chilichonse chomwe chili m'menemu. Panali mbusa wina yemwe anatha zaka 9 akulalikira buku limeneli. Buku la Aroma lili ndi ziphunzitso zambiri zimene zimaphunzitsidwa mu Chipangano Chakale makamaka mu buku la Yesaya. Mwachitsanzo Mulungu ndiye mwini mphanvu zonse ndipo chilichonse chochitikachili pansi pa ulamuliro wake. Yesaya 43:1 Mulungu ndiyemwe amatiombola ife; Yesaya 43:21 ndi 25 Mulungu adatilenga ife ndizolinga zakendipo amatiombola ife pazolinga zakenso. Yesaya 44:1-2 Mulungu adatsankha iwo amene adzawaombole. Yesaya 45:1-7 ndi nfundo yopitiridza kunena zokhudzana ndi Ukulu wa Mulungu. Tiona ziphunziso zomwezi mubuku la Aroma. Baibulo ndi limodzi kuchokera kuchokera ku Chipangano Chakale mpaka Chipangano Chatsopano.

Augustine Woyera ndi Martin Luther onse awiriwa adagwiritsa buku la Aroma kuti akonze ziphunzitso zawo zokhudzana ndi Mulungu. Luther adaphunzira kuchokera mu bukuli kuti Ntchito yamunthu siingamubweretsere chipulumutso. Ndipo kuti chimene chinaphunzitsidwa iye ndi ampingo wa Akatolika chokhudzana ndi nfundoyi ndichotsutsana ndi Baibulo. Timalungamitsidwa ndi ntchito ya ulere ya Mulungu basi. Aefeso 2:8-9.

Martin Luther amatengedwa ngati kholo la mpingo wa chiprotesitanti(mpingo wa chikonzedwe kuchoka mu katolika). Mipingo yonse imene siyachikatolika imatchedwa yachiprotesitanti. Martin anali okhumudwa kaamba kakhalidwe logulitsa zikalata za chipulumutso zomwe ampingo wa katolika amapanga panthawiyo. Makalatawa amakhulupiriridwa kuti amapangitsa munthu kukhululukidwa machimo awo. Utha kugula imodzi lero kuti udzakhululukiridwe machimo omwe udzachimwe m'mawa. Makalatawa amathanso kugulidwa kuti athandidzire munthu amene anafa kale kuti machimo ake akhululukiridwe. Martin atawerenga bukuli adaonazolakwika zomwe akatolika amaphunzitsa.

I. Chigawo choyamba cha buku la Aroma chikunena bfundo yakuti anthu onse awerudzidwa kale chifukwa cha uchimo wao. Aroma 1-3:20.

1. Paulo akuyamba kalatayi popereka moni kwa anthu,ndipo mu vesi 1 akudziulula yekha kuti iye ndi mtumwi wa Yesu. M'malonje ake Paulo akunena mu vesi ya 13 zakhumbo lake loyendera anthu akuRoma. Tikudziwa pakuwerenga buku la Machitidwe a Atumwi kuti chokhumba chake chakwaniritsidwa tsopano.

2. chaputala cha 1:14-23 tikuphunzirapo kuti Mulungu wadziulula yekha kwa anthu onse ndipo kuti anthu onse pamaso pake ndi opalamula.

A. timaphunzira mu vesi 14-15kuti uthenga wabwino siwakwa Ayuda okha ayi, komanso wina aliyense ngakhale muyuda kapena wamitundu. Uwu ndi mutu waukulu mubuku la Aroma komanso Baibulo lonse. Pamaso pa Mulungu, palibe kutsiyana pakati pa anthu amitundu yotsiyana kapena ambiri zotsiyana. Mkhristu wina aliyense kufunikira kwake ndichimodzimodzi pamaso pa Mulungu. Mbusa wa mpingo wanu sindiye kuti wayandikira kwa Mulungu kupotsa inuyo.

B. vesi 16-17 ikunena kuti titsachite manyazi ndi uthenga wabwino, chifukwa uthenga wabwinowu uli ndi malangizo omwe amatilodera kumoyo otsatha. Tiyenera kukhala muchikhulupiriro mwa Yesu Khristu. Mulungu wapereka chipulumutso koyamba kwa Ayuda kenako kwa amitundu, koma anthu ambiri anamukana Yesu nthawiyo komanso akumukana panopa.

C. vesi 17 ikutiudza kuti olungama adzakhala ndimoyo chifukwa chachikhulupiriro.

i. kuti tipite kumwamba tiyenera kulungamitsidwa ndikukhala olungama pamaso pa Mulungu. Chilungamitsi ndi ntchito ya Mulungu yokhululukira ochimwa ndikuwalandira ngati olungama pamaso pake. Pokhala olungama, kulungamitsidwa kutanthaudza kuti pamaso pa Mulungu palibe tchimo lililonse. Chilungamitso chimenechi chimachitika kamodzi pa moyo wa munthu mpaka muyaya.

ii. timakhululukidwa kupyorera mu chikhulupiriro mwa Yesu Khristu. Timalandira ichi kwaulele kuchokera kwa Yesu pakutipatsa ife chilungamo chake zomwe zimadziwika kuti kutsinthana (imputation). Chomwe chimachitika ndichakuti Yesu amapatsidwa machimo anthu onse ndipo anafa pantanda m'malo mwathu.

iii. timakhala ndichikhulupiriro muzinthu zambiri mwachitsanzo mpando womwe tikukhalira kuti ukwanitsa kutitsenza ndipo ife otsagwa. Chikhulupiriro chopulumutsa chimatanthaudza chikhulupiriro chathu ndikudalira kwathu mwa Yesu amene sitimuona ndi maso akuthupi kapena kumukhudza.

3. Paulo tsopano akuyang'ana chifukwa chomwe anthu amafunikira chipulumutso. Aroma 1:18-20 paulo akuti, Mulungu wakwiya ndi ife anthu chifukwa ndi ife ochimwiratu. Akutinso tilibe chowilingula chifukwa Mulungu wadziulula yekha kwa ife. Vumbulutso ndilomwe limatipangitsa ife kudziwa Mulungu. Liwu loti vumbulutso limatanthaudza kuika kapena kuulula chinthu chomwe chinabitsika. Ndipo vumbulutso ili limatanthaudza kuti timadziwa kuti tingapembedze Mulungu woona ndikudziwanso ndi mtima wathu chomwe ndichoyenera ndi chotsayenera kuchichita.

A. Mulungu anadziulula kwa ife munjira ziwiri. Njirazi ndi njira ya chindunji(special reveration) ndi njira yopanda chindunji(general reveration).

i.Njira yopanda chindunji. Anthu onse amaona njirayi imene timaona Mulungu akudziulula yekha kudzera mu chilengedwe. Munthu aliyense atha kuona dziko lomwe latidzungulirali. Masalmo 19:1-6; Aroma 1:19-20; 2:14-15. Mwanjira ina, chilengedwe chimapereka umboni

kuti kuli Mulungu, koma nzeru iyi paiyo yokha ndiyotsakwanira kuthandidza munthu kuti apedze chipulumutso chifukwa sitingadzindikire Khristu kudzera munjirayi. Mwanjira ina titha kuona kuti muchilengedwe muli Mulungu koma Yesu sitingamudzindikire kupyorera munjirayi.

ii. Njira ya chindunji. Umu ndimomwe timadziwira dzina la Yesu lomwe ndilofunikira pa chipulumutso chathu. Aroma 10:9-10 tiyenera kuitana dzina la Yesu kuti tipulumutsidwe. Ndivumbulutso la Mulungu kupyorera mu Baibulo lomwe limatilodzera ife njira ya chipulumutso kudzera mu dzina la Yesu.

B.Malemba ndi momwe Yesu wadziululira kwa ife. Chilichonse timadziwa chokhudza Mulungu chikupedzeka mu Baibulo. Sitingadziwe chilichonse chokhudza Mulungu popanda Baibulo. Baibulo ndi Maua a Mulungu. Lilibe zolakwika komanso ndilamphavu. 1 Akor. 2:13, 2Tim. 3:16. Baibulo ndilokwanira. Chibvumbuluso 22:18-19 kumbukirani-*khulupirirani chokhacho chimene Baibulo limanena chokhudza Mulungu ndikuphunzitsa chokhacho chimene Baibulo limaphunzitsa.*

C. vesi 20 ikutiphunzitsa ife kuti, popedza Mulungu wadziulula yekha kwa ife, tilibe chowiringula pamene tasankha kutsapembedza Iye. Tikuyenera chilango ndithu, ndovuto lathu pamene tasankha kupita ku Gahena.

E. Tiyenera tiyang'anitsitse Vesi 18 imene ikunena za mkiyo wa Mulungu. Tiyenera kuphunzitsa anthu athu zakuopsa kwa mkwiyo wa Mulungu. Tiwachenjedze iwo ndithu. Chipangano Chakale chaphunzitsa zambiri zokhudzana ndi mkwiyo wa Mulungu.anthu ambiri samafuna kunva zokhudzana ndi mkwiyo wa Mulungu. Malo mwake amafuna kunva uthenga omwe umawabweretsera chimwemwe okhudzana ndi ubwino wa iwo eni, okhudzana ndi chuma, komanso moyo wa thanzi. Onani 2Tim.4:3-4.

i. mipingo yambiri imalalikira mauthenga amene amatsangalatsa makutu kunvera. Mauthenga amene amalorera machismo ena kuti azichita monga umathanyula, komanso kutha kwa maukwati. Iyi simipingo ya chikhristu ayi.

ii. Azibusa ambiri salalikira za mkwiyo wa Mulungu chifukwa amafuna kukhala ndi mpingo waukulu kwambiri. Mulungu choyambirira amafuna mpingo Woyera kenako udzikula bwino. Amayang'ana kwambiri chiyero otsati chiwerengero.

iii. Ndiudindo wa akulu ampingo kulalikira zokhudza mkwiyo wa Mulungu. Tikukakamidzidwa kuphunzitsa anthu za ichi nthawi itsanathe kuti awerudzidwe ndi Yesu. Chifukwa china chomwe chingapangitse ife kuphunzitsa za mkwiyo wa Mulungu ndichakuti, sitinganvetsetse kuchimene Mulungu watipulumutsa popanda kunvetsetsa za mkwiyo wake. Pamene mochulukira tiphunzira za mkwiyo wa Mulungu ndipamenenso tidzakhale othokodza chifukwa Yesu anatipulumutsa ife ku gahena otsadzima.

iv. Muli ndime zambiri mu Baibulo zomwe zikutinjedza pa zithu zokhudzana ndi mkwiyo wa Mulungu, kunyatsidwa kwake, kutsiyana ndi ndime zomwe zikunena za chikondi ndi chifundochake. Muli ndime zotsachepera 600 zokhudzana ndi mkwiyo. Onani Ekso.22:22-24 ndi buku la Chivumbulutso ngati zitsanzo chabe. Mulungu akufuna kuti tichenjedzedwe molimba kotero kuti titsapite kugahena. Ndilamulo labwino kwa m'busa kulalikira za mkwiyo wa Mulungu komanso kuphunzitsa mofanana za chisomo cha Mulungu.

D. chidule cha Vesi 18-20 ndichakuti anthu onse amadziwa kuti ndikolakwika kupanga milungu yao monga mafano. Timadziwanso kuti ndikolakwika kupalamula milandu ngati ya kupha, kugwirira,kutaya mimba,kuba ndizina zotere. Kotero palibenso chowiringula

pamilandu imeneyi. Chilango choopsa chikubwera kwa onse amene apitiridza kusanvera Mulungu.

4. vesi 21-23 werengani ndi kuona chifukwa chomwe Mulungu ali okwiya ndi ife. Taona kuti Mulungu wadziulula yekha kwa ife,ndipo tilibenso chotilepheretsa kupemphera ndikunvera Iye.

A. Monga taphunzirira, anthu onse amadziwa kuti zinthu zoti ndizolakwika. Mulungu amakwiya nafe zedi chifukwa timatsankha kusamunvera Iye, tili kudziwa kuti kutero ndikuchimwa.

5. vesi 24-28 tikuphunzirapo kuti chifukwa cha kuipa komwe kuli m'mitima mwa anthu, Mulungu adawapereka iwo mu zilakolako za mitima yao. Mwanjira ina, tinganene kuti Mulungu waleka anthuwo kutsankha kuti adzingochimwirachimwirabe. Iye amalola anthu kuchita ndikutsangalala ndi tchimo lomwe akuchita. Anthu amachita ichi, koma otsadzindikira kuti pali chilango chomwe chikubwera patsogolo pao, zomwe tiphunzire mu chaputala chachiwiri.

A. vesi 26 ikutanthaudza kuti Mulungu wareka anthu kukhala mumachimo awo. Tikuona izi kumaiko a azungu kumene chaudzimu chidachoka kale koma anthu angolemereralemerelabe.

B. vesi 26 ikutanthaudzanso kuti Mulungu adzalanga anthu pakuwapatsa iwo boma lotsauka kwambiri lomwe lidzachite changu potsakadza miyoyo ya anthu. Onani Yesaya 3:1-8. Onani dziko la United States of America kuti muone boma loipa lomwe likupatsula dziko lonse.

C. Taganidzirani, kodi dziko lanu lilinso pachiweruzo?

D. tchimo la umathanyula likugwiritsiridwa ntchito ngati chitsanzocha tchimo loopsa mu vesi 26-27. Izi zikufanana ndi maiko akwao kwa azungu. Zaka 40 zapitazo umathanyula udali otsowa kwambiri ndipo amabitsa tchimo limeneli kuti litsaonekere kudziko lapansi. Panopa tchimoli lili poyera tsopano, alibenso manyazi, kudziko lonse lapansi. Anthu ochita nchitidwe oterewu akuloledwa m'maiko ambiri kumamangitsa ukwati. Akudzunzika kwambiri padziko pano chifukwa chatchimo lawoli, makamaka pa nkhani za umoyo wabwino, koma chilango chenicheni pakutsalapa machimowa chikubwera kumapeto kwa moyo uno.

i. umathanyula ndi tchimo loopsa kwambiri ndipo Mulungu amadana nalo kwambiri. Lev. 18:22 ndi 20:13 Mulungu akutsutsa kolimba za tchimo limeneli mobweredzabweredza. Ichinso chinali chifukwa chomwe adaonongera Sodomu ndi Gomora.

ii. ndichifukwa ninji Mulungu amadana ndi tchimo la mchitidwe wa mathanyula? Chifukwa choyamba ndichakuti tchimoli limaononga chikhalidwe cha chilengedwe cha ukwati. Mulungu adakhadzikitsa mabanja pamene adakhadzikitsa maukwati (Gen. 2:24). Satana akuyetsetsa kuononga mabanja. Ndipo m'maiko ambiri wakwanitsa kale kuchita zimenezi. Kodi zili bwanji zinthu izi kuno kwathu ku Africa? Mabanja kodi akadalimbabe?

6. Aroma 1:28-32 apa akubweredza ganizo lakuti Mulungu walolera iwo kupitiridza kuchimwa ndikutinso tchimo lawo likulirakulirabe mpaka pamapeto pake adzaiwala kuganidzira kuti chomwe akuchita ndi tchimo loopsa kwambiri. Sazanva mwaiwowo kuletseka kuchita choipa achiganidza, ndipo adzaiwala zotinso kudzabwera chilango. Nthawi yoyamba titasankha, kuchimwa tidzaona kuti tachita cholakwika, koma pamene tabweredza kuchita tchimoli tidzaiwala kuti ndikulakwa kutero. Machimo ena monga kunama kapena kumenya mkazi wathu sizivuta kuchita izi mobweredzabweredza; ndipo chikumbu mtima

chathu chimafa kotheratu. Mulungu amatileka kudzilakolako za uchimo wathu, ndipo amakhala oopsa kwa ife panthawiyi.

7. chaputala 2:1-5 akutiudza kuti palibe adzakkhale ndi chodzitetedzera pa machismo ake ndipo adzawerengeredwa mulandu pa tchimo lililonse. Mkwiyo wa Mulungu ukukula chifukwa cha mtima wathu wauchimowu ndipo nkhwinya ndi ululu wa chilango chake zikukulanso.

A. otsatsirira wochimwa otsalapayo amene akhala m'moyo wachitsangalalo ndi manyado. Kumbukirani nkhani ya Lazalo ndi munthu wachuma mu Luka 16; komanso werengani Masalmo 46 makamaka vesi 16-20. Tangokhazikikani pa ubale wanu ndi Mulungu wanu. Tidzakhala muyaya ndi Ambuye wathu, otsachedwa ndi chitsangalalo cha dziko lapansi chakanthawi kochepa.

8. tikuona kuti panthawi yoikika Mulungu adzalanga ochimwa wotsalapayo. Chaputala 2:6-16 tikunva kuti munthu aliyense adzawerengeredwa mulandu wake pazomwe adachita. Idzi zitanthaudza kuti Ayuda adzaweruzidwa monga m'mene ayimila mwa Yesuotsati ndi zikhulupiriro zao kapena zikhalidwe zao. Ezekieli 18:30.

A. vesi 9-11 Mulungu adzatiwerudza ife potengera zoona zenizeni za moyo wathu. Chiweruzo cha Mulungu, sichidzakhala chokondera konse ayi.

B. vesi 12-15 Mulungu adzaweruza potengera zomwe Malamulo ake amanena. Sapadzakhala chowiringula chifukwa choti sitinadziwe Malamulo ake.

C. vesi 16 ikutiphunzitsa kuti tidzawerudzidwa potengera zinthu zonse ngakhale zinthu zobitsika zomwe. Mulungu adzawerudza mtima ndi miyeso yake.

9. chaputala 2:17-29 Paulo akuyankhulanso ndi Ayuda. Akuwatsindikidzira kuti adzawerudzidwa malinga ndi ntchito zao. Ayuda ambiri amaganidza kuti chifukwa cha ubale wao wapaderadera ndi Mulungu, dzidzawathandidza iwo kuti asakawerudzidwe ndi Mulungu. Anthu onse kuphatikidzapo abusa adzawerudzidwa ndithu.

A. Vesi 17-24 Paulo akuwaudza Ayuda kuti ali ndi udindo wapadera chifukwa alangizidwa ndi lamulo kotero akuyenera kuphunzitsa anzao ndi kukhala m'moyo wa chitsanzo. Iye adawadzudzula Ayuda chifukwa amaphunzitsa lamulo lomwe iwonso amalephera kulinvera. Adawaudza kuti khalidwe lotero ndichitonzo kwa Mulungu. Tiyenera kuchita zomwe tikuphunzitsa chifukwa popanda kutero ndiye kuti ndife achinyengo.

B. Vesi 25-29 Paulo akukamba za mdulidwe umene akuufanidzira ndi ubatizo komanso akunena za umembala wa mpingo, ndipo akutsimikidza kuti zinthu izi sidzingathandidze kukhala wangwiro pamaso pa Mulungu. Tiyeni titsatire maganidzo ake mu mavesi otsatirawa.

i. vesi 25-26 akutsindika kuti mdulidwe/ ubatidzo ndichizindikiro chakunja chabe, ndipo ndichotsayenera ngati sichili muntima wamunthu. Kubatidzidwa kwanu umatsimikidzira dziko lapansi kuti inu ndi mkhristu, koma ndikhalidwe lanu lomwe lingachitire umboni kuti idzi ndi zoona. Mulungu amafuna kutiona kuti tili ndi mtima woyenera kapena khalidwe labwino lamumtima pamaso pache. Amafuna kutiona ife kuti moona tikuyetsetsa kunvera Malamulo ake. Khalidwe lanu la mumtima pamaso pa Mulungu ndiloyenera kwambiri kupotsa maonekedwe anu kwa anthu. Kodi mumakonda moyo wachikhristu?

ii. vesi 27 akuti tapatulidwa ndi zochita zathu. Munthu yemwe ndi wa Mulungu amachititsa manyazi yemwe Sali mwa Mulungu. Mwanjira ina mitundu amene anali mwa Mulungu amachititsa manyazi Ayuda omwe kapena munthu aliyense amene sanvera Mulungu .

iii. vesi 28-29 ndichidule cha ndimeyi. Maonekedwe akunja siofunikira kwambiri pamaso pa Mulungu monga m'mene ulili mtima wake. Mtima ndiomwe Mulungu akauwerudze. Munthu atha kunama kwa munthu nzake koma sanganamidze Mulungu.

Tikuona chitsanzo cha idzi kawirikawiri mu Baibulo.tiyeni tione buku la Amosi;

1. Amosi 5:11-12 akulongotsola za choipa chomwe chimachokera mumtima.
2. Vesi ya 16 ikulongotsola za chiwerudzo chomwe chidzadze chifukwa cha tchimo limeneli.
3. Vesi 21 Mulungu akunyasidwa ndi kupembedza kwa anthu amenewa chifukwa ndichipembedzo chachiphamaso otsati chochokera mu mtima.
4. Vesi 24 tikuona kuti Mulungu akufuna chilungamo komanso mtima Woyera. Tiyenera kupembedza Mulungu ndi mtima Woyera komanso wolapa.

Munthu wina aliyense anakhalako wawerudzidwa ndi ntchito zomwe anachita otsati ndi chilichonse ayi. Mkhristu wawerudzidwa ndi zintchito zochokera kwa Yesu, maka pa chikhulupiriro chake mwa Khristu. Anthu ambiri amaganidza kuti adzapulumutsidwa chifukwa anabadwa ndikukulira m'banja lachikhristu kapena amapita kutchalitchi.Monga ngati Ayuda adali ndi maganizo onga omwewa, koma adzapulumutsidwa pokhapokha pamene amanga ubale ndi Yesu.

10. Aroma chaputala cha 3.

A. vesi 1-4 kodi ndimwayi otani omwe ungabwere pamene wabwadwa ngati muyuda kapena kubadwira m'banja la chikhristu? Paulo akuyankha ponena kuti banja la chikhristu limakhala ndi chidziwitso cha zinthu zokhudzana ndi Mulungu, kotero amaphunzitsa zoona zokhudzana ndi Yesu kwa ana awo. Izi zikutanthaudza kuti munthu amene wabadwa mu banja la chikhristu ndikotsavuta kukhala nkhristu kutsiyana ndi yemwe wabadwa m'banja la chikunja.

B. 3:9-18 palibe munthu wolungama ndipo kuti tonse tawerudzidwa kale chifukwa cha zochita zathu. (Tiona zambiri za izi tikafika mu chaputala cha 9).

i.Tikuona apa za phunziro la kuchimwiratu kwa mtundu wa anthu. Izi zimatanthaudza kuti anthu onse kupatula Yesu adayetsedwa ochimwa chifukwa cha tchimo la Adamu. Mwaife kuchokera pa chilengedwe chathu mulibe chabwino. Chabwino mwa ife chimadza kuchokera kwa Mulungu.

ii. ntchito ya Mulungu Mzimu Woyera imaonekera kwa munthu payekha komanso kwa khamu/gulu la anthu. Mzimu Woyera amakhala mwa mkhristu aliyense ndipo akhristu ndi Mzimuyi amakhala ndi zotsatira zabwino pa anthu otsatembenuka mtima. Zabwino zili mwa ife zimachokera kwa Mulungu. Yakobo 1:17.

11. mavesi amenewa akutsilidza chigawo choyamba chachikulu cha buku la Aroma. Taona mfundo zitatu zikuluakulu mumavesi amenewa zomwe zikubweretsa chifupikitso cha chigawo choyamba chabuku la Aroma.

1. munthu wina aliyense ali ndi koti akayankhe pamaso pa Mulungu kutengera pazimene adachita.

2. munthu aliyense ndi ochimwa ndipo machimowa ndi otsawerengeka.

3. palibe munthu adzalungamitsidwe ndi ntchito zabwino adadzichita.

II. Tamalidza gawo loyamba la buku la Aroma lomwe limatiphunzitsa ife kuti tonse tawerudzidwa kaletsono tili okonzeka kuona gawo la chiwiri lomwe likufotokodza momwe tingalungamitsidwire. Komanso m'mene tingapulumutsidwire ndi chikhulupiriro mwa Yesu.

1.Aroma 3:21-31 kulungamitsidwa chifukwa cha chikhulupiriro. Njira yokhayo ya kuchipulumutso.

A. chilungamo cha Mulungu chikulongotsoledwa mu Vesi 21-26.

i. chavumbulutsidwa ichi pano ndipo sichikhudzana ndi lamulo. Izi zikutanthaudza kuti sitingalungamitsidwe ndi lamulo. Vesi 21.

B. chilungamo chake chikupedzeka kwa ife kudzera muchikhulupiriro cha Yesu Khristu basi, ndipo ichi chikufunika kwa anthu onse. Vesi 22-23.

i. Aroma 3:23 ndi imodzi mwa mavesi amene tiyenera kuwalowedza chifukwa pakufunika ndithu kunvetsetsa zomwe vesiyi ikutanthaudza.

C. chipulumutso ndi mphaso yaulere kwa ife, koma tiyenera kukumbukira kuti mphasoyi idali chipsinjo kwa Yesu Khristu. Vesi 24-25 mtengo wa chipulumuso chathu ndi mwazi wa Ambuye Yesu Khristu.

D. chiwerudzo cha Mulungu chimadzidzilitsidwa ndi msembe ya Yesu ndipo ngati ife tikhulupirira Yesu timupemphe iye kuti atipulumutse kenako tilape pakutero tidzalungamitsidwa ndipo tidzalandira pamapeto pake moyo wosatha. Vesi 26

E. tikuona zoona ziwiri mu vesi la 27-30

i. choyamba ndichakuti ife anthu sitichita chilichonse kuti tilandire chipulumutso, pokhala ichi kuti ndi choona palibenso chifukwa choti tidzitamandire. Khalidwe lathu likhale la chiyamiko pamaso pa Mulungu. Vesi 17-28

ii. chachiwiri tikuona kuti Ayuda ngakhale amitundu ndiofana pamaso pa Mulungu. Mulungu amationa tonse ngati ochimwa komanso ngati tatembenuka kale mtima amationa tonse Ayuda ndi Amitundu ngati anthu olungama. Izitu zikuphatikidza anthu onse amene ali padziko lapansi. Mulungu amaona chimodzimodzi anthu achifilika, azungu, aluya ndi ena otere. Vesi 28-29.

F. ndichifukwa ninji lamulo likufunikirabe? Likufunikira kuti litidzindikiritse pakati pa cholakwika ndi chabwino. Tikuona kuti munthu amalephera kutsunga lamulo mwa ngwiro, kotero lamulori limationetsa chosowa chomwe tili nacho ndicho Mpulumutsi Yesu Khristu. Vesi 31.

2. Paulo akutchula Abrahamu mu chaputala cha 4ngati chitsanzo pamfundo yakuti chikhulupiriro chathu pa Yesu chimatengera m'meneife talungamitsidwira. Abrahamu adayetsedwa olungama chifukwa cha chikhulupiriro, onani Gen.15:6 atsadachite ntchito iliyonse monga mdulidwe.

A. Abrahamu analungamitsidwa ndichikhulupiriro, vesi 1-8. Paulo adagwiritsa ntchito Abrahamu chifukwa Ayuda amamulemekedza kwambiri, ndipo amafuna kuonetsa kuti kwanthawi yaitali munthu wakhala akulandira chipulumutso kaamba ka chikhulupiriro, otsati chifukwa cha ntchito za munthu.

B. vesi 9-12 tikuphunzirapo kuti mdulidwe kapena ntchito sangapangitse ife kupedze chipulumutso.

i. vesi 11- chikhulupiriro cha Abrahamu chakhala ngati chitsanzo chakalekale kwa anthu amitundu. Abrahamu ndi tate wa anthu onse okhulupirira. Tikuona izi kachiwiri pa vesi ya 23-25. Izi zikutiudza kuti chilungamitso chimene Abrahamu adalandira ndi chaife tonse, inu ndi ine.

ii. tikuona mu vesi 11 kuti mdulidwe komansi ntchito zinabwera pambuyo ngati zipatso za chikhulupiriro. Chikhulupiriro chimatulutsa ntchito zabwino.

iii. mdulidwe wa Chipangano cha Kale unali chidzindikiro chakuti Ayuda adali ochokera kwa Mulungu. Lero mumpingo ubatidzo udalowa m'malo mwa mdulidwe ngati chizindikiro cha ubale wathu ndi Mulungu.

iv. tidzingoyerekedza mdulidwe ngati chizindikiro cha chipulumutso, otsati kuti tingapedze chipulumutso pa chimenechi monga Yakobo anena pa Yakobo 2:14 ndi 17-18. Chipulumutso chathu chimaonetseredwa ndi ntchito zabwino. Koma sintchito zomwe timachita zimene zimatipatsa chipulumutso chifukwa timapulumutsidwa ndi chikhulupiriro basi

C. Tikuona zophunzira zambiri zokhudzana ndi chikhulupiriro (vesi 16-22).

i.Okhulupirira tonse ndife ana a Abrahamu. Vesi 16-22.

ii.Vesi 18-21 tikunva zoti ngakhale Sarai mkazi wake anali okalamba kwambiri komanso otsabereka, Abrahamube adakhulupilira Mulungu, pamene adamuudza kuti adzakhala tate wa anthu.

iii.Vesi 22 ikuti chikhulupiriro chimenechi chidamupangitsa iye kuyetsedwa olungama.

D. Lonjedzo la chilungamitsochi likupitanso kwa okhulupirira onse. Mu Baibulo munthu amatengedwa kuti ali ndichikhulupiriro chopulumutsa pamene akudziwa choonadi chomwe chingamuthandidzire iye kuti apulumuke agwirizane nacho, ndikupumira pa icho komanso kudalila pa chimenecho. Chikhulupiriro chimenechi chimatsogolera ku kulapa machimo zomwe ndizofunika pa chipulumutso chathu. Ndikwabwino kudzifufudza tokha ndikuona ngati tili ndi chikhulupiriro chonga chotere.

    i. Mwanjira ina munthu amapulumutsidwa pokhulupirira kuti Yesu ndi Mulungu, pamenenso munthu afunsa Iye kuti akhale Mulungu wake, pomupulumutsa iye pamene adalira mwa Mulungu ndi kulapa machimo moona mtima.

3. chaputala cha 5:1-11 tikunva kuti pali madalitso omwe amadza chifukwa chakulungamitsidwa.

A. Madalitso omwe amadza nthawi yomwe wangolungamitsidwa

i. awa ndi mavesi omwe amanditonthodza kwambiri. Chithunzithunzi chomwe tonse tiyenera kukhala nacho ndi chakuti munthu osapulumutsidwa amakhala pankhondo ndi Mulungu. Pamene takhala mkhristu, ndipo talungamitsidwa timakhala pa chiyanjano ndi

Mulungu, osati pa nkhondo ayi. Ndimaona kuti kukhala pankhondo ndi Mulungu Wamphanvu zonse ndi chinthu choopsa kwambiri ndipo ndikwabwino mofulumira kukonza ubale wathu ndi Mulungu wathu pofuna khukhalirana pa ntendere ndi Iye ndipo ichi ndichinthu chabwino.

B. vesi 3-5 ikutsutsana ndi uthenga wotsangalatsa anthu, pankhani za chuma, umoyo wa bwino ndi zina zotere. Timanva mauthenga awa mu mipingo yomwe timapitayi. Sitikufunikira kukhumudwitsidwa ndi kutaya chiyembekedzo chathu chifukwa tikuyenda m'moyo wa msautso. Yang'anani chomwe nsautso imabweretsa pa moyo wa munthu. Mavuto amabereka chiyembekedzo mwa ife kotero timatsimikidziridwa za chipulumutso chathu. Izi zimapatsa chitsimikidzo ku chipulumutso changa.

C. vesi 6-11ikutithandidza kudziwa m'mene Yesu amatikondera. Timawerenga kuti munthu amataya moyo wake ndicholinga chofuna kupulumutsa moyo wa munthu wina yemwe akumudziwa bwino. Tangoganidzirani kuti Yesu adataya moyo wake ndicholinga chofuna kutipulumutsa pamene tidali pa nkhondo ndi iye. Mwanjira ina Yesu adatifera chikhalireni ife tidali tikulimbana ndi Iye. Uwu ndi umboni otsimikidzira mulingo wa chikondi cha khristu kwa ife.

D. Aroma 5:9-11ikutipatsa chitsimikidzo cha zinthu za nsogolo. Izi zikutiphunzitsa kuti talungamitsidwa ndi mwazi wa Yesu kotero sitidzakumana ndi mkwiyo wa Mulungu. Tinganene kuti sitidzalangidwa kugahena chifukwa cha machimo athu kwamuyaya. Vesi 10 ikutsimikidzira zimenezi ndipo vesi 11 ikutilimbikitsa kuti titsangalale pokhala pa mtendere ndi Mulungu.

E. Aroma 5:12-21awa ndi mavesi omwe akunena za Adamu woyamba ndi Adam wachiwiri (Yesu). Anthu ambiri amakana kuti Adamu adalikodi. Ife ngati akhristu sitiyenera kukana chinthu chimenechi. Sipangakhale chipulumutso ngati tingamaganidze kuti kunalibe Adamu. Tikhulupirire kuti Mulungu adalenga chilichonse ndipo zonena za asayansi kuti zinthu zidakhalako mwa okha ndizonama. Ganizo la asayansili limakana ntchito ya Mulungu kuti ndi Iye adalenga chilichonse chomwe chiliko.

i. tikuona apa kuti tchimo lidalowa mwa mtundu wa anthu chifukwa cha munthu m'modzi, ndipo lafalikira kwa onse chifukwa cha Adamu. Ndipo imfa inadza kwa munthu chifukwa cha Adamu (vesi 12-14)

ii. mavesi 15-21 tatsokera chifukwa cha munthu m'modzi koma chipulumutso chopambana chadza kwa ife kudzera kwa munthu m'modzi Yesu.

a. Mavesi18-19 kuchimwa kwa munthu m'modzi kunadzetsa chiwerudzo kwa ntundu wonse wa anthu ndipo chilungamo cha munthu m'modzi chinabweretsa chilungamitso ndi moyo wotsatha.

b. Vesi 20-21 akutionetsa tchutchutchu wa tchimo kuti ndi chiyani, ndipo pamene tchimo likukulirakulirabe chisomo chimakhala chikupita pa tsogolo ndipo chisomo cha Mulungu chimakhala chachikulu kupotsa mphamvu ya tchimo. Palibe tchimo lomwe ndilalikulu pamatso pa Mulungu limene tsangathe kulikhululukira. Kumbukirani kuti tchimo ndi chilichonse tikunena kuganidza ndikuchita chomwe sichikondweretsa Mulungu. Ndichilichonsenso chomwe Mulungu amafuna chomwe tsitichita, tsitinena kapena kuganidza.

III. AROMA 6-11 zinthu zatsintha tsopano chifukwa uthenga wabwino walalikiridwa kwa ife. Siifenso akapolo a tchimo,koma tsopano titha kukhala m'moyo wokondweretsa Mulungu, zomwe tsitikadakhodza kudzichita chifukwa tidali mu uchimo.

1.Aroma 6:1-11 mbuye wa kale ndi mbuye wa tsopano.

A. Paulo akufusa mfunso mu vesi 1-2. ngati kukhala m'moyo wa ngwiro sichipulumutso nanga ndichifukwa ninji tiyenera kukhala mwachitsanzo. Ndichifukwa ninji sitikungoyenera kutsangalala m'moyo wathu wa uchimo. Yankho la Paulo ndilakuti sitingakhale m'moyo wa uchimo ngati tinafa kuuchimo. Mkhristu sachimwa mwadala. Mkhristu nthawi zonse amakondwera pamene asangalatsa Mulungu, kotero sangafune ndipang'ono pomwe kukhumudwitsa Iye.

Paulo mumavesi omwewa akuyankhapo pa maganidzo oti mkhristu atha kukhala m'moyo ngati otsapulumutsidwa kuti izi zitha kukhala zachisoni koopsa. Chimodzi mwa ubwino wakukhala mkhristu ndichakuti moyo wathu umayenda munjira zomwe zimakondweretsa mulungu. Ngati titsankha kukhalabe m'moyo wauchimo ndiye kuti tikudzitsutsa tokha kuti tili ndi Yesu. Mwanjira ina, pamene tasintha chikhalidwe chifukwa pokhala mu njira zokondweretsa Mulungu ndi chizindikiro choti tili mwa Yesu ndipo kuti ife ndi ana ake.

C. Paulo wayankhula za mphaso yaulele ya chisomo, ndipo anthu ena amanena kuti chomwe tiyenera kuchita ndikungolandira mphasoyi ndikukhala m'moyo womwe tingakonde. Paulo muchaputala cha 6, akuyamba kuphunzitsa kuti nkhistu akuyenera kuyenda munjira zoonetsa kuti ali ndi mbuye watsopano. Tinvere Mulungu ndikuonetsanso kuti tsitili muukapolo ndi tchimo.

2. Paulo tsopano mu mavesi 12-14 akutiudza momwe tingapangire izi. Tinazolowera kukhala akapolo a Satana ndi tchimo. Pano tsopano tikutumikira mbuye watsopanondiye Mulungu ndipo izi zili chomwechi chifukwa cha Yesu. Ndiye njira yabwino yokana kuchimwa ndi kudzipereka kwa nthunthu kutumikira mbuyeyu. Titsalole mbuye wakale kutimamatira chifukwa tsopano tikuyang'aniridwa ndi mbuye wasopano. Tiyetsetsa m'mene tingathere kukondweretsa Mulungu.

A. tchimo lidzakhalabe mwa ife, koma pamene tidza chifupindi Mulungu, ndipamenenso tidzafunafuna kudana ndi tchimoli mwa chisomo cha Mulungu. Izi ndinjira zomwe tingapangire zinthuzi.

i. peweni mayetsero. Ngati kuredzera, kumwa mankhwala odzungudza bongo kapena chiwerewere ndi vuto pamoyo wanu, talikiranani ndi anthu omwe amakonda kuchita zinthu zimenezi.

ii. phunzirani mu zolakwika zanu zakale ndikupempha Mulungu kuti akuthandidzeni pamene muyetsedwa kuti mugwe mu uchimo.

3. kuyambira mu Aroma6:15-23Paulo akubweredza chomwe anakamba pa chiyambi cha mutu wa 6 kuti ndichifukwa ninji tinvera lamulo pamene sitingapulumutsidwe nalo. Paulo akuyankha funsoli pofusanso funso lomwe akuliyankha ndi yankho lophweka.

A. vesi 16 paulo akunena kuti mbuye wathu ndiyekhayo yemwe tiyenera kumutumikira.kunvera kwathu ndi umboni oti ndi ifedi opulumutsidwa.

B. vesi 21 ikutiudza kuti ngati akhristu ndife amanyazi chifukwa cha machimo athu ndipo kuti machimo athu amatilodzera kuchionongeko.

C. vesi 22 ikunena kuti ngati ndiifedi akapolo a Mulungu, tidzapitadi kumoyo wotsatha.

D. Aroma 6:23 ndi imodzi mwa mavesi oti tilowedze. Ikuti timalandila imfa yotsatha chifukwa cha chamachimo athu. Koma Yesu akupereka kwa ife moyo wotsatha ngati mphaso yaulere ngati tili ndi chikhulupiriro mwa Iye.

Muchaputala cha 7:1-6 Paulo akukamba za momwe banja limathera pa imfa ndikumupanga m'modzi okhala ndi moyoyo kukhala waufulundikukwatiranso kawiri ngati ali ndi chikhumbokhumbo chimenecho. Akupheredzera nkhani imeneyi kuti pamene takhala mkhristu sitikhalanso alamulo (vesi 6). Ndife omatsuka kulamulo ndi omangika kwa Mzimu.ganizo loti ndife omatsulidwa kuchilamulo limatanthaudza kuti lamulo silidzatitsutsanso. Koma tiyenera tinvere Malamulo onse khumi, koma pamene tawaphwanya iwo sikuti tidzawerudzidwa kwa muyaya chifukwa cha chimenechi.

A.kuti tisasokonedzeke tiyeni tionenso zomwe Paulo adanena zokhudzana ndi ufulu komanso ndi udindo kuti tisachimwe.

i. palibe kukayika kuti, mkhristunso amagwa muuchimo, koma tchimo sichikhumbokhumbo kapena chizindikiro cha mkhristu.

ii. lamulo limathandidza kuyetsa muyeso wa tchimo. Okhulupirira woona amadziwika ndi kutsunga lamulo.

iii.mkhristu woona amasunga lamulo otsati ngati ntchito koma chifukwa cha chikondi. chitsanzo chabwino ndi ntchito zabwino zomwe timzchita kubanja kwathu otsati chifukwa ndiudindo wathu kutero komanso kuti ndi chikondi chomwe tili nacho pa banjalo.

5.chaputala cha 7:7-25 tikuonapo za za moyo wakale ndi watsopano wa mkhristu.

A. Aroma7:7kachiwiri akuti cholinga cha lamulo ndikudzindikiritsa tchimo. Palibe cholakwika ndi lamulo. Vesi 12 ikutiudza kuti lamulo ndiloyera. Vuto lili ndi ife chifukwa tilibe chabwino champhavu mwa ife kuti tisunge lamulo.

i. cholinga cha lamulo ndikulekanitsa pakati pa chabwino ndi choipa, ndipo limatithandidza ife kuona kuti sitingathe kuchita kabwino pamaso pa Mulungu. Ndipokhapo pamene tazindikira kulephera kwathu kuti tingafunefune mpulumutsi.

6. Aroma 7:14-25 akulongotsola za za kulimbana pakati pa thupi lathu la uchimo lomwe limafuna kutsatira zokhumba zake, ndi chudzimu chili mwa ife chomwe chimafuna kunvera Mulungu. Ndikupyorera muchithandidzo cha Mulungu, kuti tingakhodze kuchita chinthu chabwino. Kulimbana uku kudzakhalapo mpaka mathero a moyo wathu uno. Pamene mkhristu, pang'ono ndi pang'ono alimbikitsa moyo wathu tidzakhodza kuchita chabwino kawirikawiri. Ichi ndi chimodzi mwa zifukwa zotipangitsa ife kuwerenga Baibulo lathu ndikuphunzira m'mene tingathere zinthu zokhudza Mulungu.

A. tidzalimbana ndi tchimo nthawi zonse pamene tikadali ndi moyo.

B. chifupikitso cha zomwe takambazi. Ife akhristu sitidzawerudzidwa kapena kutsutsidwa ndi lamulo. Lamulo lidaikidwa kuti litilodzere ife kuchipulumutso maka muchikhulupiriro mwa Yesu Khristu. Chomwe tingachite ngati alaliki ndichomwe achikonzedwe amakedzana amachita chomwe amati tiphe munthu ndi lamulo ndikumudzutsa iye ndi uthenga wabwino. Izi zimatanthaudza kuti tiphunzitse anthu athu za kutsokera kwawo ngati adalira ntchito zomwe amachita kuti zingawagulire chipulumutso. Tiwaphunzitse za kutayika kwawo ngati alibe mpulumutsi. Dziwani kuti Achikonzedwe amakedzana amanena za akhristu amene

amadziwa Baibulo bwino lomwe. Amene anali mbadwa zoyambirira za dziko la United states of America.

7. chaputala 8:18-39 akufotokodza zokhudzana ndi Masauso-chiyambi cha ulemerero.

A. tikuona mu vesi 18 kuti tipirire mavuto amoyo uno chifukwa tili nditsogolo labwino lomwe likutidikirira. Tikuonanso kuti tiyembekedzere kuvutika koma masauso amenewa ndi akanthawi kochepa ndipo adzatitsogolera kupita kumwamba. Kwa ife nsautso imaoneka chinthu chachikulu kwambiri, koma sikanthu tikayerekedza ndi mphoto yomwe ikudzawo.

i. Paulo adali katakwe potilangidza ife za masautso chifukwa iye mwini adazunzika kodetsa nkhawa chifukwa cha uthenga wabwino, onani 1Akor.11:23-28. Akutitsogolera ndi chitsanzo otsati mau chabe.

Paulo adali msogoleri wamphavu- wakhala chitsanzo kwa ife.

B. mavesi 19-27 akunena za kubuula kwa mitundu itatu; onsewa akudza chifukwa cha zotsatira za tchimo la Adamu. Monga adamu, tchimo lathu limavulaza anthu ena.

i. kubuula koyamba tikukuona mu vesi 19-22 pamene tikunva kuti masauso adzolengedwa zonse, monga nyama, akubwera ngati zotsatira za tchimo la Adamu.

ii. mavesi 23-25 akunena za kubuula kwa munthu komwe kukudza ngati dzotsatira za tchimoli.

iii.mavesi 26-27 akunena kuti Mzimu umabuulanso m'malo mwathu. Amatipempherera pakupereka moyenera mapemphero athu kwa Mulungu Atate. Kumbukirani kuti Mzimu ndi nthandidzi wathu.

C. pano tili ndi zifukwa zitsanu ndi chimodzi zomwe zikupangitsa ife kukhala ndi chisangalalo cha tsiku ndi tsiku (vesi 28-39).

i. vesi ina yoti tilowedze ndi Aroma 8:28. Chimene amatanthaudza apa ndichakuti tikhulupirire Mulungu, ndipo tidzatonthodzedwa mumayetsero onse tikudutsamo. Kodi mukuvutika chifukwa chaululu wa ngozi yomwe inakugwerani? Tonthozekani podzindikira kuti nsauso yanuyo ikuchitika kuti ikakubweretsereni ubwino ku moyo wanu. Sitinganvetsetse chifukwa chomwe timazunzikira, komanso kuti ndichifukwa ninji kuti zinthu zili monga m'mene zililimo, koma Yesaya 55:8 akutiudza kuti Mulungu saganidza monga ife timaganidzira. Tikhulupirire Mulungu. Onani Gen. 50:20 kuti muone phunziro lofana lokhudza Mulungu kuti amachita zinthu kuti zitibweretsere ife ubwino.

a. zinthu ziwiri izi zimatithandidza kukhululukira ena ndikuiwala zoipa zomwe ena atichitira. Gen. 50:20 tikuona kuti Yosefe adakhululukira abale ake ndi mtima wake wonse.

ii. mavesi 29-30 akutiudza kuti timasangalala chifukwa Mulungu adzatenga anthu ake kupita nawo kuulemerero. Sadzalephera kupita nafe kumwamba.

Iii. vesi 31 ikuti Mulungu ali mbali yathu ndipo pachifukwa ichi, adani athu sadzatigonjetsa.ndikwabwino kukhala ndi wamphanvu kumbali yathu amene ali Mulungu.

iv. vesi 32 ikuti Mulungu adapereka mwana wake kwa ife pakutero adzatipatsa chilichonse tikufuna monga chisomo, chilimbikitso ndi kumwamba.

v. ife akhristu sitili otsutsidwa (vesi 33-34) chifukwa cha ntchito ya Yesu Khristu.

vi. timatsangalala chifukwa (35-39) cha chikondi chopotsa cha Mulungu kwa ife. Chikondichi ndichachikulu kuti chidzatitengera kumwamba ndipo palibe yemwe adzatilekanitse ife ndi Khristu. Onani vesi 37 ndipo kumbukirani kuti ndinu Agonjetsi. Zinthu zokhoma m'moyo mwanu zitsakugonjetseni, chifukwa kupyorera mwa Yesu ndi ife opotsa agonjetsi. Yesu amafuna kutitidzikhalandi chikhulupiriro pa Iye ndikutsangalala kuti tili ndi Iye.

8. chaputala 8 ndi ndime yamphavu mu Baibulo, komanso chaputala cha 9 Paulo akutipatsa chithunzi cha chisoni. Chisoni cha anthu omwe akutayika amene atidzungulira. Paulo amanena za Ayuda koma ndi ife lero tinena za anasi komanso anzathu omwe tayandikana nawo Nyumba, banja lathu ndi ena otero.

A. Paulo muchaputala cha 9:1-5 akuonetsa kuti adakonda Ayuda anzake, kwambiri kuti akadalolera kupereka malo ake akumwamba bola ngati msembe imeneyi ikadakhala yololedwa kutero pofuna kupulumutsa Ayudawa. Kodi timakonda anthu otsapulumutsidwa amene azungulira ife ndikukhala ndi njala yogawana nawo uthenga wabwino, kuti akalangidwe okha pakunyodzera kwao?

i. Mbusa wa chikhristu ali ngati Paulo. amakonda anthu kwambiri kuti amadzipereka msembe kwa iwo. Mwaufulu amawapempherera iwo, nagawana nawo zomwe iye alinazo.

B. mavesi 10-18 ndi nfundo zoonetsa ukulu wa Mulungu. Timanva kuti iwo asanabadwe, Mulungu adakonda Ykobo nada Esau. Vesi 15 adzachitira chifundo amene iye afuna ndipo vesi 18 adzaumitsa mitima ya iwo waafuna kuwaumitsa mitima.

C. Paulo akutiudza chifukwa chimene Mulungu adatsiya otsapulumutsa Ayuda m'malo mwake kumakapulumutsa amitundu. Akunena muvesi 30-33 kuti Ayuda anakangalika kudzipulumutsa okha ndi ntchito zao maka ponvera lamulo komanso pochita mdulidwe, ndipo adakana kulandila Mulungu ndikuvomeredza kuti njira ya chipulumutso kuchokera kwa Iye ndi kukhala ndi chikhulupiriro mwa Yesu. Ayuda adali ovuta kuwatsogorera (Yesaya 30:1) monga momwe tilili ife lero. Anthu ndiodzikudza amafunafuna njira zaozao m'malo mwa njira za Mulungu.

9. chaputala cha 10 ndichaputala chonena za umishonale.

A. Paulo adayamba mu vesi 1-4 kulongotsola khumbo la chipulumutso kwa Ayuda anzake. Adayankhula za change cha Ayuda pamaso pa Mulungu, koma adakangalika kuchita zinthu munjira yaoyao m'malo mwa njira yoyenera yomwe ndikudzera mwa Mulungu. Vesi 4 monveka bwino ikuti khristu ndiye yankho lathu.

B. mavesi 9-10 akufotokodza momwe munthu angapulumutsidwire. Izi ndizotsavuta kuzinvetsetsa. Timapulumutsidwa ndi chikhulupiriro mwa Yesu ndi kudalira Iye pa chipulumutso chathu. Mulomo utanthaudza chomwe chimachoka pakamwa pathu chimafotokodzera chomwe chili mkati mwathu. Ngati Yesu alidi muntima mwathu, chomwechonso zoyankhula zathu kwa ena, zizalingana ndi amene ali mumtima mwathu.

i. chitsanzo cha izi ndikunena kwa anzathu za kukhala mkhristu.

ii. chitsanzo china ndipamene tilalikira uthenga kwa onse.

C. tikuona mu vesi 11-13 Mulungu ndi Ambuye wa Ayuda komanso amitundu ndipo pamaso pake palibe kutsankha. Ana onse a Mulungu amawadalitsa chimodzimodzi.

E. vuto ndilakuti wina atha kumaudza otsapulumutsidwa za chipulumutso mwa Khristundipo akhristu ambiri alibe chidwi chofalitsa uthenga. Uthenga wa vesi 14-21 ndiwakuti alaliki akufunika kufikira anthu otayika. Iyi ndi ntchito ya nkhristu aliyense.

Monga vesi 14 ikunenera kodi munthu angakhulupirire bwanji munthu amene sananvepo za iye, ndipo vesi 15 ikuti kodi wina angawaudze bwanji za Yesu pokhapokha wina atatumidzidwa kwa iwo.

i. izi zikutanthaudza kuti anthu ena adayitanidwa kutsiya kwawo kukakhala mamishonale kumadera achilendo.

ii. Otsalawo akuyitanidwa kukhala kwao komweko ndi kukhala alaliki komwe iwo aliko. Akhristu onse ndi mamishonale. Titha kupita kapena kupemphera kapena kutumidza ena kuutumiki.

iii.pali madalitso kwa anthu amene amafalitsa uthenga wabwino umene umapedzeka mu Yesaya 52:7. Munthu amene amathandidzire kuti wina atumidzidwe kukakhala mishonale amadalitsidwa pamodzi ndi mishonaleyo.

F.vesi 16 ikuti siyense amanva uthenga wa Mulungu kuti akapulumutsidwa. Ndintchito yathu kugawana ndi ena uthenga wabwinowu, koma Mulungu adzakhudza anthu omwe ndioona.

G. tikuona muvesi 17kuti Mau a Mulungu (Baibulo) ndilofunikira pa chikhulupiriro. ndimuBaibulo momwe timaphunzira za Yesu ndi chipulumutso kudzera mwa Iye. Kumbukirani kuti chilichonse timadziwa chokhudzana ndi Mulungu chimapedzeka mu Baibulo; osakhulupirira chilichonse cha Mulungu pokhapokha titachiwerenga kuchokera mu Baibulo.

H. chifupikitso chanzonsezi ndichakuti, munthu angapulumutsidwe pokhulupirira ndi podalira mwa Yesu. Ndikofunikira ife kuudza otsapulumutsidwa za Yesu kuti Iye ndi ndani. Akhristu onse ndi udindo wao kufalitsa uthenga wa Yesu, ndikutumidza ma mishonale kukalalikira uthenga wabwino kumadera onse a dziko lapansi. Timatumidza mamishonale powapempherera ndi kuwathandidza pa chuma. Mkhristu aliyense akuyenera kukhala mulaliki komanso kuthandidzira mamishonale ngati satero ndiotsanvera.

10. Chaputala cha 11 chikunenanso za Ayuda.

A. vesi 1-2 Paulo akufunsa ngati Mulungu waakana Ayuda ndikusankhaamitundu. Paulo akuyankha funsoli ponena kuti izi sizoona chifukwa iye mwini ndi Muyuda amene walandilanso chipulumutso. Kotero pali Ayuda ena pakali pano amene ndi akhristu enieni.

B. vesi 25-32 akupitiridza kukamba za Ayuda m’moyo walero komanso m’mene adzakhalire m’moyo wa nsogolo.

i. vesi 25 Paulo akunena kuti kuumitsa ntima kwadza pakati pa ana a Israeli zomwe zikutanthaudza kuti Ayuda ena ali ndi mitima yofewa kuti alandire moyo wotsatha ndipo akumalowa muchikhristu, pamene enawo aumitsa mutima yao ndikukaniratu kulandira uthenga wabwino.

ii. vesi 26 ikupereka mwayi wazokambirana ndi msunso. Pali malingaliro awiri omwe ndi otsiyana.

a. Ena amati vesi 26 imakamba za mfundo yakuti njira yokhayo yomwe Ayuda kapena aliyense angapulumutsidwe nayo ndi kudzera mwa Muyuda-Yesu Khristu.

b. Ena amati vesiyi imakamba za zansogolo pamene padzakhale unyinji wa Ayuda otembenuka mtima matsiku amsogolo, Yesu asanadze kachiwiri. Palibe anganene kuti akulongotsola zoona, kapena ayi.

C. mavesi 33-36 tikuona Paulo akuyimba Nyimbo ya chiyamiko chifukwa cha chikonzero chabwino cha Mulungu pa chipulumutso. Tiyeneranso kuchita chimodzimodzi.

III. CHAPUTALA CHA 12-16 tikuona kupheredzera kwa maphunziro amene tawaona mu chaputala cha 11 kumoyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Kodi tingakhale bwanji m'moyo wa chikhristu komanso kuti tingalandire bwanji mphaso yayikulu ya chipulumutso.

1. Chinthu choyamba chomwe tikuchiphunzira mu 12:1 ndichakuti tiyenera kuyeretsa ndi kupereka moyo wathu kwa Mulungu pomutumikira Iye. Mwanjira ina, tiyenera kutenga kutumikira Mulungu ngati cholinga chachikulu m'moyo wathu. Tidzipereke kwa nthuthu kwa Mulungu. Akhristu akuyenera kukhala otsiyana ndi ndi maonekedwe adziko lapansi.

A. ife akhristu tipembedze ndi kutumikira Yesu m'mene tingathere ndi mphanvu zathu zonse. Mulungu amakondwera pamene pamene tidzikhuthula ndi mtima wonse kwa Iyekutsiyana ndim'mene amanvera tikamamupatsa zinthu ngati ndalama. Tiyenera kudzindikira kuti ndife a Mulungu, ndipo tifunefune kutsanzira Yesu muzonse adachita kutsiyana ndi kutengera zochita za dziko lapansi. Tidzipemphera kuti tikhale ofanana ndi Yesu. Tikhale otanganidwa ndi zinthu za Yesu.

2. vesi 3-8 ikunena za mgwirizana wa mpingo. Ife akhristu ndi mbali ya thupi limodzi, kotero tiyenera kugwira ntchito limodzi pogwiritsa ntchito mphaso ndi kuthekera komwe tilinako ulemerero wa Mulungu ndi chipindulo cha wina aliyense. Akhristu ali a m'banja limodzi, kotero tiyenera kutengapo mbali pachilichonse chochitika ku chalichi.

A. vesi 3 ikutiudza kuti tidzifufudze tokhandikuona mphaso kapena luso lomwe Mulungu adatipatsa kuti timutumikire Iye ndi anthu ena. Asangothamanga kupanga chiganidzo kuti muli ndi mphaso ya ubusa. Pempherani ndikufunafuna chitsimikidzo cha Mulungu pamphaso mukuikayikirayo. Kodi mumadziwa mpaso yanu?

B. mavesi 4-5 akutiphunzitsa kuti mpingo wa Khristu ndi thupi limodzi, ndipo limagwira ntchito bwino ngati chiwalo chilichonse chitengapo mbali pathupilonselo. Thupi lonse lamunthu limagwira ntchito bwino pamene ziwalo zonse zikuthandidzirana kutumikira thupilo. Ndipo izi ndi chimodzimodzi ndi chikhalidwe cha mpingo.

C. mavesi 6-7 akutiudza ife m'mene tingagwiritse moyenera mphaso yomwe tili nayo kuchokera kwa Mulungu kuti ithandidzire anthu ena.

3. mavesi 9-21 akupereka mphunziro za m'mene mkhristu angachitire.

A. 9-10 akuti tiyenera kukhala ndichikondi chenicheni kwa wina ndi mzake. Tiganidzire anzathu kopotsa kudziganidzira tokha. 1 Yohane 4:11-12.

B. vesi 11 osangokhala duu;kangalikanipotumikira Mulungu.tili ndi moyo umodzi okha ndiko kukhala kwa Mulungu.

C. vesi 12 khalani nthawi zonse chifupi ndi Mulungu powerenga Baibulo ndi kupemphera.

D. vesi 13 chilimikani kuthandidza anzanu oyera mtima amene akutsowa.

E. vesi 14 ikutipatsa malangidzo okhudzana ndi m'mene tingayendere m'moyo wa masautso umene akhristu adzayenera kupilira. Malangidzo ena ndikudalitsa iwo akutinzunza zomwe zili zotsiyana ndi m'mene ife timakhalira. Chomwe timakwanitsa kuchita ndi kuvulaza yemwe akutidzunza. Koma Baibulo likuti dalitsani iwo okuzunzani. Mateyu 5:44 ndi Luka 6:28.

F. Vesi 15 ikulimbikitsa kukhala okangalika ndi moyo wa anzathu. Titseke pamene akutseka ndipo tilile nawo pamene akulira ndipo tichilimike nawo pamodzi pamene ali mu nsauso monga m'mene unalili mipingo otsautsidwawo (Ahebri 13:3)

G. vesi 16 ikutilimbikitsa kukhala mogwiridzana ndi wina aliyense. Timutenge wina aliyense chimodzimodzi ndipo tasanyodzetse munthu ngakhale ali otsika bwanji. Zilibe Kanthu kuti ndiwe mbusa wankulu kwambiri, koma ukuyenera kuchita ndi munthu wina aliyense mwa ulemu. Mulungu amaona mkhristu wina aliyense chimodzimodzi. Miyambo 3:7ndi langizo labwino kwambili.

H. Mavesi 17-19 akutiphunzitsa kukhala muntendere ndi anthu onse. Iwalani za munthu yemwe wakuvulazani ndi kukuwawitsani mtima. Otsaganidzira kubwedezra choipa, tsiyani zonse m'manja mwa Mulungu, pewani kupsa mtima.

I. mavesi 20-21 akupereka malangizo okuya kwambiri. Gonjetsani adani anu ndi chikondi pamene alimbana nanu. Otsabwedzera choipa kutsinthana ndi choipa.

4. chaputala cha 13 chikutiphunzitsa kukhala mbadwa zaulemu. Tikulimbikitsidwa kunvera Malamulo a mudziko ndi kunvera olamula. Palibe olamulira wadziko amene adzazuze akhristu chifukwa Baibulo limaphunzitsa kuti tidzidula misonkho.

A. ganizo muvesi 1-2 ndilakuti boma limatenga ulamuliro wake kuchokera kwa Mulungu, kotero kuti iye amene anyodza boma akunyodzanso Mulungu.

B. pali nthawi zomwe sitiyenera kunvera boma. Iy ndi nthawi pamene boma likutilamula kuchita zinthu dzotsutsana ndi Mau a Mulungu (Mac.4:19 ndi Mac 5:29). Mwachitsanzo

i. Aroma adalamula mzika za mziko mwao kulambira kupembedza msogoleri wao ngati iya ndi Mulungu. koma akhristu adatsutsana ndi lamuloli.

ii. Ku America tchalitchi chikulamulidwa kutenga ochita umathanyula kugwira ntchito ndi ana aakhristu.

iii.boma limatha kulamula mbusa kulalikira zinthu zotsemphana ndi Baibulo.

C. mavesi 3-4 tikunva kuti boma lilipo kuti litibweretsere ife ubwino. Kotero ndichabwino boma kutipatsa chilango pamene taphwanya lamulo ngakhale chilangocho chili choti ife tiphedwe. Tiyenera kunvera boma lathu.

Mutha kuona m'mene zinthu zingavutire ngati boma palibe. Taonani ku Somaliya. Anthu ambiri kumeneku akuzunzika koma boma likulephera kutetedza anthu akugwira ntchito yopereka chakudya kwa anthuwa, kotero kuti otsowa chakudyawa sakuthandizidwa. Ana akumangofa chifukwa cha njala. Somaliya ndi maiko onse akufunika maboma a chikhristu.

D.Aroma 13:5-7 ikutipatsa zitsanzo zenizeni za momwe tinganvere Malamulo. Tikulimbikitsidwa kunvera malamulo ndi kukhoma misonkho.

i. Pamene mulingalira za malangizo am'Baibulowa okhudzana ndi kunvera lamulo komanso kupereka msonkho, funso limkhala lakuti ndichifukwa ninji maboma ambiri amazunza akhristu. Ife akhristu ndi mbadwa zaulemu mudziko.

F. vesi 8-9 ikutiphunzitsa ife kuchita ndi wina aliyense mwa chikondi. Apa Paulo akubweredza zomwe Yesu adanena kuchokera ku Marko 12:31.

G. Aroma 13:10 akufotokodzera za chikondi ndipo akuti chikondi chimenechi chimatsangalatsa mulungu.

H. vesi 11-14 akutiudza ife kuchita changu pokhala m'moyo woyenera chifukwa kubwera ka chiwiri kwa Yesu kwayandikira ndipo nthawi ikuthamanga. Nthawi monga vesi 11 inena yayandikira kutsiyana ndimomwe linalili dzulo. Nthawi iliyonse tidzikhala ngati ndi tsiku lomalidza.

5. chaputala cha 14 ndi phunziro la moyo watsiku ndi tsiku momwe tingakhalire muntendere ndi anzathu komanso tiphunzira za umodzi wa mpingo. Komanso tikunva kuti akhristu ambiri amakhala ndi maganizo otsiyana pazinthu zomwe apatsidwa kuti achite chifukwa sachita izi ndi motsogoreredwa ndi Mulungu. Mbale wolimba ndithu atha kuganidza kuti, ngati chinthu china sichiletsedwa moonekera ndiye kuti ndichabwino kuchichita. Mwachitsanzo, wina atha kuganidza kuti ndichotsalakwika kumwa kachasu, kapena mzimayi kuvala buluku mutchalitchi kapena kupita kukaonera sinema kapena kupita kudansi. Mbale ofoka atha kuganidza kuti zinthu zimenezi ndizoletsedwa. Ndiye tikuona muchaputala cha 14 kuti mu mpingo woyamba chimodzi mwa zinthu zomwe samagwiridzana ndi zinthu zodyedwa ndi zotsadyedwa. Phunziro ndilakuti titsamatsutsane pa zinthu zing'onozing'ono. Baibulo likutipatsa ufulu wambiri mu madera otsiyanatsiyana.

A. vesi 1-6 ikutiudza kuchita zomwe tingathe kuti tikhale muumodzi ndi anzathu. Titha kunyalanyaza zinthu zomwe ndi zotsafunikira kwenikweni. Ngati tikufuna titha kupanga nsutso pazinthu zina koma pamapeto tisadane koma tikhalebe abwenzi. Cholinga chathu chikhale kuyendera limodzi ngati kungakhale kotheka.

i. vesi 1akutiudza ife kumulandira munthu otsutsana naye ngati mbale ndi ulemu. Mulandireni monga m'mene iye alili ndipo otsayetsera kumutsintha. Lemekedzani abale ofoka.

ii. vesi 2-3 akutiudza kuti timulemekedze potsamupeputsa iye. Titsazitengere pa mgong'o zinthu zimene ndizosafunikira kwenikweni. Chisanzo ndi ichi kuti mfrilika kuphunzitsa mfirika mzake ndi udindo wa mkhristu wina aliyense, potsayang'anira zipembedzo. Iyi ndi mfundo ya bwino ngakhalenso m'banja.

iii.vesi4-5 otsamuwerudza iye (Mateyu 7:1)

iv.vesi 5 onetsetsani kuti chomwe mukuchita ndi cholondola.

v.vesi 6ikutikumbutsa kuti mbale wina aliyense akuyenera kuchita chomwe angathe pofuna kulemekedza Mulungu.

B. vesi 7-9 kumbukirani kuti cholinga chathu ndi kutsangalatsa Mulungu. aliyense achite ndi cholinga choyenera-mitima yathu ikhale yoyera.

C. vesi 10-12 tikuudzidwa kuti titsadziike tokha owerudza wa anzathu. Mulungu ndiye owerudza wathu. Tikhudzike ndi zochitz zathu chifukwa aliyense akawerudzidwa ndi zinthu zomwe adachita pamatso pa Mulungu.

D. mavesi otsatira mu chaputalachi akunena za umodzi pakati pa wina ndi mzache. Tisakhale chopunthwitsa munjira ya anzathu. Izi zikutanthaudza kuti sitiyenera kupanga zinthu zomwe zingachimwitse ena. Chitsanzo cha izi ndikuimba Nyimbo mokwedza zomwe anthu ena zimawaipira zomwe zingawapangitse kufuna kukumenya iweyo. Otsatsuta pamatso pa munthu amene amaletsa kutsutako.

E. chitsanzo chabwino muphunzirori ndi ubatidzo. Ubatidzo suzapulumutsa aliyense kotero tiyenera kupewa makangano pankhani ya kabatidzidwe. Pali nfundo zabwino pa ubatidzo wa ana. Komanso pali nfundo zomveka pongochita ubatidzo wa akulu okha. Aliyense abatidze monga aonera kukhala koyenera. Koma titsadzudzule iwo amene abatidza motsiyana ndi ife. Tilemekedze maganidzo a wina aliyense pa nkhani imeneyi. Titsutse panfundo zomwe sizigwiridzana ndi Baibulo monga kulimbikitsa kuti munthu atha kupulumutsidwa ndi ntchito zake. Tiyenera kutsutsa zotere ndi mtima wolimba kwambiri.

6. CHAPUTALA CHA 15 chikupitilidza maganidzo a chaputala cha 14. Aroma 15:1-13 akunena dza chikondi cha pa abale. Paulo akuyamba mu vesi 1-6 kuyankhula ndi akhristu olimba komanso akhristu ofoka.

A. Zinthu zitatu kuti zichitike

i. olimba akuyenera kuthandidza otsalimba vesi 1.

ii. vesi 1ikutiphunzitsa kuti sitikuyenera kuchita zinthu zotsangalatsa ife eni, koma choyambirira titsangalatse Mulungu ndipo kenako anthu ena otere.

iii.vesi 2 ikutiudza kuthandidza ena powamangilira.

B. zifukwa zopangira zinthu izi vesi 3 ikuti tikutsatira chitsanzo cha Yesu.

C. zotsatira pachikhalidwe chimenechi;

i. vesi 2 ikuti izizatilimbikitsa kuwamangirira anzathu.

ii. vesi 6 ikutiudza kuti izi zidzadzetsa umodzi mu mpingo.

iii.vesi 6 ikutiudzanso kuti umodzi umenewu udzapititsa patsogolo ulemerero wa Mulungu. cholinga chenicheni m’moyo wathu ndi kulemekedza Mulungu ndikukondwera mwa iye nthawi zonse.

D.choncho mu vesi 7-13 Paulo akuyankhula Ayuda ndi amitundu. Akutiudza kuti ndi cholinga cha Mulungu kuti onse akapulumutsidwe kotero kuti pamodzi akalemekedze Mulungu. Masalmo 117:1

E. Paulo akuyamba kulemba zokhudzana ndi iye mwini. Akunena za ntchito ya Mulungu yomwe anayenera kugwira. Adali mishonale wa kwa Ayuda ndipo wagwira ntchito m’malo motsiyanasiyana pofalitsa uthenga wa Mulungu komwe uthengawu sunalalikidweko. akuyankhula za pulani yake yopita ku Aroma podzera ku Yerusalemu. Tikudziwa kuchokera mu buku la Machitidwe kuti adapita kwa Aroma, koma otsati mu njira imene iye adakonza.

8. chaputala 16:1-16 Paulo akunena za anthu otsiyanatsiyana pamene amatsilidza kalatayi.

A. Paulo kachiwiri akupereka chenjedzo kwa ife kuti tidziwe zoti pali anthu ena omwe adzayetsere kulekanitsa mpingo kotero asawalorere iwo. Vesi 17-18 akuti anthu amene

amadza ndi mgawaniko mumpingo satumikira Mulungu koma akudzitumikira okha.onani 3Yohane 1:9.

B. vesi 16 ndi phunziro la kamatsulilidwe ka Baibulo. Paulo satanthaudza kuti tikuyenera kumaphyophyonana wina ndi mzake. Akutanthaudza kuti tiyenera kupatsna moni wina ndi mzake mwa chikondi malingana ndi chikhalidwe cha deralo.

C. mau otsilidza mu buku la Paulo kwa Aroma ndi chiyamiko, kwa Mulungu. Mipingo yambili imatsilidza chipembedzo chake ndi mau a mdalitso kwa anthu kuchokera kwa Mulungu. Awa ndi mau amdalitso otengedwa kuchokera mu Baibulo. Izi zinayambika mu Numeri 6:22-27. Mau awa amatchedwa Mdalitso, ndipo ndikwabwino kuchita chinthu ichi komanso sikoyenera kutsachita ichi. Ichi ndi chimodzi mwa zinthu zomwe ndi chitsanzo cha zinthu zomwe Baibulo limatipatsa ufulu kuchita m'mene tikuonera kuti ndi zolondola.

## 1 AKORINTO

Paulo adalemba bukuli akukhala ku Aefeso, mzinda omwe umatchuka kuti ku Turkey m'matsiku aleroli. Adalembera ku mpingo omwe udali mu mzinda wa ku Giliki otchedwa Akolinto omwe udali olemera kwambiri. Kalatayi idalembedwa ndicholinga chokonza mavuto omwe adali mumpingomu, ndi kulimbikitsa umodzi.

Chaputala cha 1-6 Paulo akuyankhapo pa nkhani yokhudzana ndi mpingo

1.Paulo akuonetsa poyera kuti adarembera kalatayi ku akhristu a ku Akolinto mu vesi 2 pamene akupereka moni kumpingowu ndipo adawalimbikitsa iwo. Akuwadziwitsa kuti ngakhale akukonza mavuto mumpingomu komabe akuwalimbikitsa iwo. Mkhani ndiyakuti ngati mufuna kupereka chidzudzulo kwa mkhristu nzathu, mukuyenera kumukondabe ndi kumutsamalira iye. Chidzudzulo cha mumpingo chimakhala kubwedzeretsa mbale ku chimwemwe cha mkhristu.

2. Vuto loyamba lomwe Paulo akuliyankhula mu chaputala 1:10-17 ndi mpanduko nkati mwa mpingowo. Akutsamalira potsatchula dzina la wina aliyense, koma vuto ndi lakuti anthu otsiyana adadziika okha kukhala atsogoleri ndipo adagawanitsa mpingo. Paulo akuti mpingo ukhale ngati mkhristu yemwe sali ogawanikana. Paulo apa akunena za vuto lotchuka la mumpingo pamene anthu amaiwala kuti iwo simutu wa mpingo ndipo kudzikudza kwao amakhala akudzipanga okha ngati mutu wa mpingo.

3. Vesi 18-20 tikuphunzira kuti uthenga wabwino ndi chinthu choputsa kwa iwo amene sakhulupirira Yesu. Osakhulupirira amaganidza kuti ife akhristu ndi oputsa.

A. Tikuphunzira muvesi 25 kuti kuputsa kwa Mulungu ndi kwanzeru kupotsa nzeru za munthu ndipo kuti kufoka kwa Mulungu ndikwamphavu kutsiyana ndi mphavu za munthu. mwanjira ina Mulungu amakhala Woyera ndi wamphanvu kutsiyana ndi ife.

4. Paulo akumalidza chaputala choyamba akunena za chitsangalalo cha Mulungu pamene agwiritsa ntchito anthu ofoka kuti agwire ntchito yake. Ngati tigwira ntchito ndi mphavu zathu tisayembekedzere chipambano,ndipo vesi 27 ikuti tidzachita manyazi. Ndikudziwa kuti chipambano chilichonse chimene ndatsangalala nacho, ngati nkhristu wantchito chabe ndichifukwa choti zachitika zonse ndi thandizo la Mulungu.

A. tiyenera kuchita monga vesi 31 ikunenera kuti tidzikudze mwa Mulungu ndi mphnvu zake chifukwa iye ndi gwero la mphanvu yathu. Ife anthu siamphanvu kopotsa kugwira ntchito

mopindulitsa ndi kuchilimika mwa ife tokha. Mulungu amatsangalala pogwiritsa ntchito anthu ofoka kuti iye, Mulunguyo awonekere kuti amachita zinthu zazikulu ndipo akuyenera ulemerero. Onani nkhani ya Gidiyoni mu buku la Owerudza chaputala 6-8

5. Paulo akupitilidza muchaputala 2:1-5 popereka chitsanzo pa nfundoyi momwe mphavu za kulalikira kwa Paulo sidzinachokera mwa iye mwini ngati odziwa kuyankhula;m'malo mwake mphanvuzi zimachokera kwa Mulungu. (vesi5)

A. Nthawi zambiri alalikira koopsa ndiomwe amakhala otsadziwa kuyankhula. Jonathan Edward amatengedwa ngati olalikira woopsa kwambiri, koma amayankhula motsapatsa chikoka. Analalikira ulaliki otchedwa, "Ochimwa m'manja mwa Mulungu okwiya" umene ndi ulaliki omwe palibe mbusa adalalikira motero, ndipo adalalikira ulalikiwu ali kudwala. Anthu ambiri adabwera kwa Yesu chifukwa cha uthengawu. Ndipo udapangitsa anthu kuyamba misonkhano ya chitsitsimutso. Kwa zaka zopitirira 200 uthenga umenewu ukumabweretsa anthu ambiri kwa nkhristu. Mphnvu mu ulaliki umenewu zimachokera kwa Mulungu.

B. Paulo akuphunzitsa mu vesi 2 kuti uthenga omwe akuphunzitsa ndi wa khristu yemwe adapachikidwayo. Munali mphavu mu uthenga umenewu, ndipo ndi uthenga womwe alaliki ayenera kulalikira.

6. Mbali ina ikutiphunzitsa kuti timanvetsetsa zokhudzana ndi Mulungu kuchokera kwa Mulungu (vesi 6-14). Mzeru za uzimu ndi zobitsika kwa iwo omwe ali otaika monga vesi 10 ikunena ndipo imaululidwa kwa ife ndi mphavu ya Mzimu Woyera. Amaulula za zinsisi za m'Baibulo kwa ife pamene tiwerenga ndi kuphunzira Baibulo.

A. vesi 11-12 tikuphunzira kuti ndi mkhristu yekha amene anganvetsetse Baibulo. izi zili chomwechi chifukwa Mzimu Woyera amatithandidza ife kunvetsetsa Baibulo ndipo ife akhristu ndi tokhafe amene tili ndi Mzimu Woyera mkati mwathu.

7. chaputala 2:14-3:3 Paulo akunena za anthu a mitundu itatu.

A. vesi 14 ikunena za munthu wa kuthupi yemwe ndi otsapulumutsidwa.

B. kachiwiri akunena za anthu auzimu vesi 15-16 amene amadziwa mau a Mulungu ndipo ndi okhwima mu mzeru za Khristu-kumvetsetsa zimene Khristu amatiphunzitsa ife. Munthu ameneyi kawirikawiri amawerenga Baibulo lake ndikutaya nthawi yaitali mukupemphera, komanso ndikusonkhana ndi akhristu anzao. Mulungu amakhala chinthu nchofunikira kwambiri m'moyo wao.

C. chaputala 3:1-3 ikunena za munthu amene wapulumutsidwa koma sadziwa zinthu zambiri za Mulungu. Munthu ameneyi sawerenga kawirikawiri Baibulo, kotero sadziwa zambiri zokhudzana ndi Mulungu. anthu otere ndi ochuluka kwambiri ndipo amayambitsa mavuto ambiri mumpingo chifukwa amachita ngati otsapulumutsidwa. Mkhristu ameneyi atha kukhala mbusa koma, chifukwa choti sanvetsetsa Baibulo amapititsa mpingo wake kuchionongeko. Chinthu chabwino ndikukhala ndi mpingo umene anthu ake amawerenga mwachidwi Baibulo kawirikawiri.

A. Munthu amene tinena apayi amalowererana ndi munthu amene amapita kutchalitchi mowirikidza ndikudziyerekedza ngati ndi mkhristu weniweni, koma ndi otsapulumutsidwa. Anthu otsapulumutsidwa amadzetsa mavuto mumpingo ndipo akuyenera kukhala nawo chidwi powatsutsa. Ndimunthu yemwe akunenedwa pa Mateyu 7:21-23.

8. Paulo akutseka ndime imeneyi ya phunziro la kugawanikana mu mpingo popempha anthu mumpingo kugwirira ntchito ya Mulungu limodzi.

9. mu chaputala cha 5 Paulo akukamba za chigololo zomwe anadziwitsidwa ngati limodzi mwa machimo amene adali mu mpingo wa ku Akolinto. Ili ndi tchimo lonyatsa kwambiri lomwe ndi vuto lenileninso mu mpingo wa lero. Paulo pa vesi 13 akutiudza kuti tiwachotse anthu oterewa pakati pathu. Tiyenera kuwatulutsa mumpingo anthuwa ngati sakulapa ntchimoli.

10. chaputala 6:1-8 chikutiphunzitsa kuti asamathamangire kukhoti pofuna kuthana wina ndi nzake. Tikambirane ndikuthetsa zovuta zathu mumpingo mamwemo. Vesi ya 7 ikuti ndikwabwino kukhala ngati ife ndi oludza kutsiyana ndikumutengera m'bale wathu kubwalo la kunja.

A. tikuona mu chaputala 6:2-3 kuti ife akhristu tiyenera kuwerudza dziko lapansi pamodzi ndi angelo , kotero tiyenera kuthesa kusanvana kwathu mkati mwa mpingo, otsati kukamang'ala kubwalo la akunja.

11. Paulo tsopano akutembenukira mu vesi 9-20 kutsutsana ndi za chikhalidwe chonyansa maka chigololo.

A. Vesi 15 ikunena kuti matupi athu ndi mbali imodzi ya Khristu ndipo titsalipange kukhala mbali ya hule. Timakhala ngati hule pamene talumikidzana ndi yemwe amachita zinthu izi. Ili ndi tchimo lomwe lili mkati mwa thupi lathu. Chigololo ndi lomwe limatsutsana ndi thupi lathu la ife tokha; funsani munthu yemwe ali ndi Edzi ngati zomwe tinenadzi ndi zabodza.

B. vesi 19-20 tikuphunzira kuti tikuyenera kutsamalira thupi lathu, chifukwa matupi athu ndi kachisi wa Mzimu Woyera amene amakhala mwa ife. Tikuona kuti sitili a ife tokha koma koma tili a kwa Mulungu chifukwa anatigula ife pa mtengo wa patali, ndipo Yesu adapereka dipo lonse. Ngati tikunvetsetsa izi tidzatsintha makhalidwe athu ndipo m'malo mokhala ngati tili a ife tokha tidzakhala tikutsiya chili chonse m'manja a Mulungu.

Chaputala 7-16 akunena za mavuto amene mpingo wa kukolinto udapempha Paulo kuti aperekepo malangizo.

1.chaputala 7:1-16 kachiwiri tikuwerenga zokhudzana ndi malangizo a m'banja komanso zoyenera pankhani ya kugonana. Phunziro pa nkhaniyi ndi lotsiyana ndi zinthu zomwe dziko lapansi limakhulupirira, koma ndi njira zomwe Mulungu amafuna anthu ache azichita.

A. Dziko limakhulupirira kuti palibe cholakwika pa nkhani ya kugonana ngati anthu akuluakulu avomeredza kutero pamene Baibulo limati tiyenera kulowa m'banja. Pakadali pano ku America kafukufuku akuonetsa kuti anthu ochuluka sakhulupirira za kulowa m'banja. Ili sikhalidwe la chikhristu.

B. lamulo loyamba lomwe tikuliona mu chaputala 7 ndilakuti kugonana sikuyenera kuchitika kunja kwa banja. Paulo akuonetsa kuti anthu amakhala ndi zilakolako za kugonana ndipo palibe cholakwika ndi chinthu ichi, Mulungu ndiyemwe amatipatsa zilakolako zoterezi. Vesi 2 ikuti ndikwabwino kukwatira ndikuthetsa zilakolakozi. Paulo akutipatsa ndondomeko imene ikuti mwamuna ndi mkazi ali ndi udindo kwa wina ndi nzake pankhani ya kugonana. Tikuona kuti onse mwamuna ndi mkazi ndi ufulu. Ndichipembedzo cha chichikhristu chokha chomwe chimatsamalira ufuluwuwa mkazi. Azibambo amaganidza kuti iwo ndiye angamapange ziganizo, koma tikuona apa kuti izi sidziyenera kukhala choncho.

C. Vesi 8-9 sivuto munthu kutsakwatira ngati zilakolako zake sizimulola kutero, koma ayenera kukwatira ngati ali ndi zilakolako akwatire basi. Vuto lalikulu kwa azungu ndi ampingo wa katolika amene amaletsa ansembe kukwatira. Ndipo ansembe ambiri amakhala akuchita nchitidwe wa kugonana mozemba ndi anyamata komanso atsikana. Ndinkhani yamanyazi mumpingo komanso tchimo lotchuka ku America ndi kumaiko a azungu. Mulungu amalola abusa kukwatira.

D. Paulo akupitirira potipatsa Malamulo ochuluka pa nkhani ya mabanja pamene okhulupirira ali m'banja ndi otsakhulupirira. Titsalekane m'banja. Tikuyenera monga vesi 16 inena; kupangitsa wachikondi otsakhulupirirayo kukhala mkhristu. Mkhristu atsatsiye otsakhulupirirayo. Tikumaona kuti abusa komanso akhristu ambiri samanvetsetsa chiphunzitsochi. Amaganidza kuti ngati wina wasintha kukhala mkhristu akhodza kuchotsa yemwe simkhristuyo. Koma Mulungu akuti tikhalebe muukwati. Tsitiyenera kutsintha chinthu chomwe tachipanga kale.

2. chaputala 8 ndichiphunzitso chomwe nthawi ino tiyenera kuchitsiya kaye. Chifukwa tilibe vuto lakudya nyama yoperekedwa nsembe mu madera athu. Komabe pali zomwe tingaphunzire pa chaputalachi. Vesi 13 ndiphunziro kwa ife. Tayankhula kale kuti tisakhale chokhumudwitsa kwa mbale yemwe ndi ofoka mu chikhristu. Paulo mu chaputala cha 9:19-23 akunena kuti tiyenera kukhala ndi chidwi chopereka ufulu wathu ngati ndikotheka kutero kwa mbale yemwe ndi ofoka.

A. Chitsanzo ndichakuti tisamwe mowa pamene apali mbale ofokayi chifukwa atha kukhala chiledzerere.

B. chitsanzo china chomwe Paulo akunena tikuchiona muchaputala 9:20. Tipewe kupangitsa munthu kukwiya chifukwa tikunena za chipembedzo chake pofuna kumuitanira kwa Khristu. Nkhani ili m'musiyi inakambidwa ndi muhindu wina amene adalowa chikhristu. Monga muhindu amakhulupirira kudya nyama ndi tchimo. Koma atakhala anaona kuti sikolakwika kudya nyama. Komabe samadya nyama pofuna kulemekedza banja lake. Pachiyambi abambo ake adamunyodza iye chifukwa cholowa chikhristu, koma pamapeto pake, abambo akewo adalowa chikhristu, chifukwa cha khalidwe lomwe nyamatayo amaonetsa kwa makolo ake padzikhulupiriro zao ngati achihindu.

3. chaputala 10:14 chikutichenjedza ife kutalikirana ndi iwo amene amachita zopanda pake, monga kupembedza mafano, kapena chiwerewere, ngakhalenso kuledzera. Chitsanzo apa ndikupewa iwo amene amapembedza mizimu. Kodi kachasu amakuika m'mayetsero? Khala kutali ndikomwe amatchedzako kachaso. Kodi umayetsedwa ndi mzimayi wina wake? Ntalikire iye.

A. vesi 13 ikutiphunzitsa kuti tisalodze chala wina aliyense pamene tagwa mutchimo. Ntchimo lililonse talichita ndilathu ndithu. Wina aliyense amayetsedwa pa nthawi yake. Ngakhale Yesu khristu adayetsedwanso. Sitchimo pamene tikana kugwa m'mayetserowa. Tikuwerenga apa kuti tisalodze munthu chala pamene tagwa muuchimo, khaya ndi Satana kapena mzathu. Mwachitsanzo, osada munthu patchimo lako lachigololo chifukwa chinali chitsankho chako kuchita tchimolo. Ngati uli ndithu mwa Mulungu, kulimbana ndi mayetsero, vesili likuta Mulungu adzapereka populumukirapo kuti ubitsale kutchimoli. Adamu analodza chala pa Hava chifukwa cha tchimo loyambalo, ndipo Hava naye analodza chala pa njoka.

4. chaputala 11 chikuyamba ndikuyankhula za kukhala tcheru ndi zochitika mu za chikhalidwe. Zikhalidwe za nyengo ya Chipangano Chatsopano azimayi amalimbikitsidwa kuvala mpango kumutu kwao panthawi ya chipembedzo. Azibambo tsamayenera kuvala kena

kalikonse kumutu panthawiyi. 1 Akor. 14:34 akuti azimayi sayenera kuyankhula mumpingo. Lero pali kutsiyana pakati pa anthu ngati zinthu zimenezi zikuyenera kuti zizichitikabe mumpingo. Anthu ena amanena kuti Malamulo amenewa sayenera kulimbikitsidwa matsiku alerowa chifukwa amanena za chikhalidwe cha Ayuda. Ndipo anthu ena amati malamulowa mkoyenera kuwatsatira chifukwa ali m'Baibulo. Ichi ndichitsanzo cha zinthu zomwe tiyenera otsalimbana nazo kwambiri pamene ena akudzichita. Iyi sinkhani ya chipulumutso ayi, kotero titsiye aliyense apemphere komanso ndikuchita zinthu monga iye aonera kukhala zoyenera.

A. Chaputala 11 chili ndi malangizo akathithi okhudzana ndi Mgonero Wa Ambuye, umene umatchedwanso kuti chiyanjano cha oyera mtima. Monga tikuphunzirira tiona zomwe sakalamentiyi imachita ndizomwe siingachite.

B. Sakalamenti ndi chizindikiro komanso chitsindikidzo cha ubale wa chipangano chathu ndi Mulungu. Chitsindikidzo chili ngati umboni omwe umaonetsa kuti ubale wathu wa chikhristu umadziwikanso ndi Mulungu. Chimapangitsa ubalewu kukhala opambana.

C. Mgonero wa Ambuye sikuti umafuna kukhutitsa thupi lathu ayi. Siumapangitsanso chodzizwitsa chili chonse monga, kuchiza matenda kapena kutipangitsa kuti tilemere.

D. Mgonerowu umatilimbikitsa ndikubweretsa dalitso pamene tikukumbukira za ubale wathu ndi Yesu Khristu. Ndipamenenso timakumbukira za nsembe yomwe Mpulumutsi wathu Yesu adaipereka chifukwa cha ife.

E. Tiyeni tione malangizo kuchokera m'malemba;

i. vesi 24 ikuti mkate umaimirira thupi la Khristu limene linanyemedwa pantanda chifukwa cha ife. Mkate umenewu siusintha kukhala china chili chonse.

ii. vesi 27 ikuti chikho chimaimirira mwazi wa Yesu umene anakhetsa pantanda chifukwa cha ife. Vinyo uja sasintha kukhala chilichonse.

F. vesi 27-30 ikutichenjedza ife kuchita nawo mgonero moyenerera. Tipange nawo mgonero pokhapokhapo tilidi akhristu, ndikunvetsetsa chomwe tikuchita. Ndiudindo wa mpingo kuona anthu osakhulupirira ndi ana amene sanvetsetsa za ichi kuti asakhale nawo mu mgonerowu. Tikuchenjezedwa kudziyetsa tokha titsadafike kugomeku. Mwachitsanzo ngati tikukhudzika ku tchimo lomwe sitidalilape, kapena tili pa disipulini (chidzudzulo) kapena kukhudzika pa mkangano ndi okhulupirira mzathu, kotero si ifenso oyenera kutenga nawo gawo la mgonero.

5. Chaputala cha 12 chikunena za mphatso ya uzimu. Paulo akunena zina mwa mphatso za uzimuzi koma osati zonse. Onani Aroma 12:6-8, ndi Aefeso 4:11 kuti muwerenge za mphatso zina.

A. vesi 7 ikuti mkhristu wina aliyense ali ndi mphatso yochokera kwa Mulungu, ndipo tikuyenera kuigwiritsa ntchito popindulitsa mpingo. Paulo sadanene kuti mphatso imodzi ndiyomwe ili yopambana kupotsa inzake. Munthu amene amatsamala mutchalitchi ndiofunikira chimodzimodzi ndi mbusa. Zimatengera thupi lonse kugwira ntchito limodzi kuti mpingo wa Mulungu upite patsogolo.

B. kutsowekera kwa athandidzi mumipingo ina zimapangitsa mbusa kutsagwira ntchito yake bwino. Mkulu wampingo amatsowekera omuthandidzira kuti achite ntchito yonse ya pa mpingo. Mose adaphunzira izi kuchokera pa malangizo a Yetero mu Eksodo 18. Akulu amalephera kugwira ntchito yao bwino kotero adawatsankhira athandidzi awo, onani Mac. 6:1-5. Akhristu onse athandidzirepo pa ntchito ya Mulungu, mumpingo.

6. chaputala cha 13 chimatchulidwa kuti chaputala cha chikondi. Werengani chaputalacho ndikutsatira malangizo. Chilichonse tikuchita kwa Mulungu ndi chabe ngati palibe chikondi.

A. vesi 1-3 tikuphunzira kuti chikondi ndi chinthu chofunukira kwambiri pa ntchito yathu ya chikhristu. Ntchito yathu imakhala ndi tanthaudzo pamene ichitika mwa chikondi.

B. vesi 4-7 akulongotsola za mitundu ya chikondi.

C. vesi 13 ndiyotsangalatsa kwambiri chifukwa tikunva kuti chikondi ndi chopotsa chikhulupiriro ngakhale chiyembekezo. Ndichifukwa ninji zili chomwechi? Chifukwa choyamba chitha kukhala choti chikondi ndi chotsatha kutsiyana ndi chikhulipiriro, komanso chiyembekezo chomwe chidzatha pamene tidzidzapita kumwamba.

7. muchaputala cha 14 tikuudzidwa za kagwiritsidwe ntchito koyenera ka mphatso zomwe tili nawo, monga uneneri, komanso malilime. Kagwiritsidwe ntchito kamphatso zathu moyenera ndipamene mphatso zathuzo zipangitsa kumangilira mpingo otsati kumatsula.

A. vesi 1 ikunena za uneneri ngati ofunukira kwambiri. Uneneritu apa akutanthaudza kuphunzitsa. Kuphunzitsa Mau a Mulungu kwa anthu ndichinthu chofunikira kwambiri.

B. chachiwiri ndichokhudzana ndi malilime. Tiyeni tione vesi 26-33 kuti tidziwe ntchito zake. Dziwani maka vesi 27. Tikuona apa kuti Mulungu adawalangidza kuti omatsulira akhalepo ngati palibe patsakhale malilime. Vesi 33 ndi 40 ikutiudza kuti Mulungu amagwiridzana ndi ndondomeko otsati chitsokonedzo.

8. Chaputala cha 15 chidalembedwa kuti chikonze ziphunzitso zomwe ndi zolakwika. Vesi 1-4 tikuphunzira kuti tikhulupirire zoti tidzaukitsidwa kwa akufa monga m'mene Yesu adaukira kuthupi.

A. vesi 5-11 akunena za mfundo yakuti anthu ambiri adaona Yesu oukayo. Kuti tikhale mkhristu, tiyenera kuvomeredza kuti adauka kwa akufa. Ndiponso ife tidzauka kwa akufa.

B. vesi 12-20 ikutsutsa kuti ngati ifeyo sitidzadzukanso ndiye kuti Yesu sadauke kwa akufa. Izi ndi zachitsoni ndipo ife akhristu tiyenera kunveredwa chisoni chifukwa tikukhulupirira chinthu chomwe sichingachitike koteronso tilibe chiyembekedzo. Vesi 20 ikunena mwamphanvu kuti Khristu adauka kwa akufa chotero titsangalale chifukwa cha mzukiro wathu womwe ukubwera kutsogoloko.

C. vesi 29 sitimainvetsetsa bwinobwino. Pali kutsagwiridzana kwakukulu pakati pa ophunzira a Baibulo chifukwa cha vesi imeneyi. Tanthaudzo leneleni la vesi limeneli linatithawa zaka 2000 zapitazo ndi zikhulupiriro za chikhalidwe zina.

D. Paulo akutiphunzitsa mu chaputala cha 15:40-44 za thupi la munthu. vesi 40 ikutiphunzitsa kuti tili ndi matupi awiri; lina ndi lapansi pano ndipo lina ndi lakumwamba. Vesi 42 ikunena kuti thupi lathu latsopanolo lizakhala lotsaonongeka, lizakhalako mpaka muyaya. Vesi 43 ikuti lidzakhala thupi la mphanvu kwambiri. Vesi 44 lidzakhala thupi lanyama komanso lidzakhala thupi la uzimu.

E. vesi 50-58 tikuphunzira kuti pamene Khristu adzabweranso, akhristu adzauka m'manda mwao ndi akhristu adzakhale ndimoyo panthawiyi adzauka kukakumana ndi Khristu, ndipo matupi athu adzatsandulika kukhala atsopano.

F. vesi 55 ikubweredza maganidzo a Yesaya komanso Hoseya kuti imfa yagonjetsedwa. Mbola yake yachotsedwa.

G. chaputala ichi chikutha ndi mau achilimbikitso kwa ife kukhala okhulupirika ndikutumikirabe ufumu wa Mulungu, chifukwa pali cholinga chofunikira kwambiri pakutumikira kwathu ndipo izi sidzidzapita pachabe.

## AKORINTO WACHIWIRI

Paulo adalemba bukuli poonetsa kukondwa kwake chifukwa cha kulapa kwa mpingo wa ku Kolinto. Komanso akukamba za ulamuliro wake ngati mtumwi wotsankhidwa ndi Mulungu.

Chaputala 1-2:11 Paulo akutetedzera za khalidwe lake. Izi zikuchitika pachifukwa chakuti atsogoleri achikhristu nthawi zina amaputidwa, ndipo tiyembekedzere chinthu chimenechi. Chidzindikiro choti utumiki wathu ukuyenda ndipamene Satana akuugwededza pogwiritsa ntchito anthu ake.

1.chaputala 1:1 Paulo koyambirira akunena kuti ulamuliro wake umachokera kwa Mulungu.

2. vesi 3-11 tikunvapo za masautso a Paulo. akutiudza za matsautso adakumana nawo. Mu vesi 10 akunena kuti adatetedzedwa mu zonsezo ndi Mulungu. Muvesi 9 akunena za phunziro mu izi kukhala kudalira kwa Mulungu otsati kwa iye yekha.

Pali zambiri zokhudzana ndi matsautso mu chaputala cha 11-12

1.tikuona kuti Paulo adazunzika chifukwa cha uthenga wabwino. Werengani 11:23-29. Tikonzekere kudzunzika monga Paulo adachitira.

2. tikuona 12:7-10 kuti Paulo adazuzikanso ndi mavuto ena. Paulo adati izi zinamupangitsa kukhala otsanyada; kunena kuti mavutowo adamupanga iye kukhala odzichepetsa.

A. tikuphunzira mu vesi 8-9 kuti ngakhale Paulo adapempha Mulungu kuti achotse mavutowa, Mulungu adakana kutero. Mulungu adamuudza Paulo kuti amudalire Iye kumuthandidza kugonjetsa mavuto ndikupitirira kumutumikirabe Iye. Sitingapereke dandaulo lililonse kuti sitili chikwanekwane kutumikira Mulungu chifukwa tikuyenera kumudalira Iye kutipatsa zonse zomwe timafuna kuti timutumikile.

B. onani khalidwe la Paulo muvesi 10 ndipo pemphani Mulungu kukupatsaninso khalidwe ngati lomwero. Ndi khalidwe loyenera kwa akhristu.

3. tikuphunziranso mu matsautso a Paulo kuti munthu sangazichidze yekha chifukwa cha mphanvu zake. Paulo amakwanitsa kuchita zizizwitsa koma analephera kudzichidza yekha.

Chaputala cha 2:12-chaputala 9 Paulo akudzitetedzera pa utumiki wake.

1.muchaputala cha 3:6-18 akunena za pangano la tsopano. Taphimbika maso mpaka Yesu atadza kudzachotsa chatiphimbacho kuti motero tidzatembenukire kwa Iye. Monga vesi 16-18 ikunena tingaone ulemerero wa Mulungu ndipo tingatsinthike kukhala muchifanidziro cha Yesu. Izi zikutanthaudza maganidzo oti ife akhristu timayamba kuoneka ngati Khristu ndipo cholinga chathu ndiko kukhala ngati Iye mochulukira chulukirabe. Chidzindikiro chotsimikidza kuti ndife mkhristu ndichakuti timasintha ndipo timaona zipatso za Mzimu mwa ife. Agalatiya 5:22-23.

2. muchaputala cha 4:2 Paulo akunena kuti waphunzitsa Mau a Mulungu mokhulupirika monga m'mene Mulungu akunenera. Tiyenera kuchita zomwezo zomwe zikutanthaudza kuti titsansinthe tanthaudzo la Mauwa pofuna kutsangalatsa anthu. Choyamba tifunefune kutsangalatsa Mulungu.

3. chaputala 5:1-10 akunena Paulo za momwe samaopera imfa. Vesi 6ndi 8 akunena chifukwa chomwe Paulo saopera imfa. Kutengera vesi 6 pamene tili ndi moyo timakhala kutali ndi Ambuye. Ndipo vesi 8 akuti pamene tamwalira timakhala pafupi ndi Mulungu. mkhristu saluza Kanthu pamene wamwalira. Chifukwa nthawi yomweyo amapita kukakhala ndi Mulungu Kumwamba.

A. vesi 9-10 tichite m'mene tingathere kuti tikondweretse Mulungu chifukwa tidzaima ndi kuwerudzidwa ndi Iye pazonse zomwe tidachita. Akhristu sadzalangidwa chifukwa cha zomwe adachita. Koma adzalandira mphoto pazabwino zomwe adachita. Tidzalandira mphoto yathu m'mwamba. Baibulo limaphunzitsa kuti, pali mphoto yolingana ndi zomwe munthu udachita. Onani Marko 10:29-30 ndi Chiv. 22:12.

4. chaputala cha 5:17 ndi vesi yolimbikitsa kwambiri. Izi ndi zina zomwe tikuphunzira kuchokera mu vesili;

A. ganizo loyamba ndilakuti pokhala kuti ndife olengedwa atsopano, munthu wakale mwa ife wachotsedwa tsopano. Machimo onse akale akhululukidwa. Palibe Kanthu kuti tinali woipa bwanji titsanalowe kwa Khristu, koma tsopano ndife okhululukiridwa, ndipo ndife anthu atsopano. Tangoganidzirani kuti Paulo adali woipa bwanji atsanatembenuke mtima.

B. ganidzo lina ndilakuti ndife olengedwa atsopano ndipo tiyenera kukhala ngati olengedwa atsopano. Tikhale ndi makhalidwe oonetsa kuti tili mbali imodzi ndi Yesu. Kumbukirani kuti takamba kale izi mu chaputala cha 3:16-18 pamene timanena kuti tidzikhala ooneka ngati Yesu m'moyo wathu wonse. Akhristu onse adzioneka kutsithika m'makhalidwe awo kutsiyana ndi kale, pamene akukula muchikhulupiriro.

5. chaputala cha 6:14-18 pali phunziro lofunika kwambiri kwa ife;

A. vesi 14 ikutiudza kuti titsayanjane ndi otsakhulupirira. Izi zikutanthauza m'banja, mumabizinesi, komanso m'mpingo.

i. miyambo ya mabanja kumaiko a azungu ndiyotsiyana kwambiri ndi ku Africa ndipo nthawi zambiri akhristu amatsankha kukwatira kapena kukwatiwa ndi munthu yemwe simkhristu.ili ndi tchimo lomwe limatitsogolera ku mavuto ambirimbiri maka pamene mwayamba kubereka ana.

ii. Mkhristu atsayanjane ndi yemwe Sali mkhristu chifukwa zikhalidwe zathu ndi zotsiyana komanso tili ndi ambuye otsiyananso. Ambuye a mkhristu ndi Yesu pamene ambuye a wachikunja ndi Satana.

iii.tionetsetse mpingo wathu kuti utsakhale paubale ndi anthu otsapulumutsidwa. Titsalole anthu amenewa kuyankhula nkhani ina iliyonse kwa anthu athu. Tionetsetse kuti choona chokha ndichomwe chikulalikidwa ndi kuphunzitsidwa kumipingo yathu.

B. onani pa vesi 16 yomwe ikuti ife ndi kachisi wa Mulungu Mzimu Woyera kotero sitingayanjane ndi akunja. Izi zikutanthaudza munthu wachikunja kuphatikidza milungu yake pa Mulungu woona amene ali mwa ife.

C. vesi 17 titsakhale muubale wa ponda ndipondepo ndi anthu otsapulumutsidwa. Ndipo vesi 18 ikuti tili ndi Mulungu ngati Atate wathu kotero titsamange banja ndi munthu osakhulupirira, kapena kuchita malonda ndi anthu otere, kapena wotsakhulupirira kukhala bwenzi la mpingo wathu.

i. tiyenela kukhala ndi ubale wina wake ndi otsakhulupirira kuti tiwalalikire iwo.

6. muchaputala 8-9 kupereka ndalama kuntchito ya Ambuye. Pamene tikuphunzira mphunziro limeneli, Paulo amakamba ndi anthu otsauka ndipo amawapempha iwo kuthandidza ena. Yesu amayembekedza anthu ake kuthandidza mpingo ndipo tikuwerenga mu buku la Luka 21:1-4 kuti anali okondwa ndi nsembe ya mzimayi wa masiye. Kupereka ndi dalitso komanso ndi mphatso yochokera kwa Mulungu. kumbukirani kuti Yesu satsowa mphatso zathuzo. Masalmo 24:1 ndi 50:10-12. Iye ali ndi chilichonse.

A. chaputala 8:1-7 ndi chitsanzo cha bwino chamomwe Mulungu amafunira kuti mpingo udzigawirako zina zomwe ulinawo. Tikuona mpingo wa ku Makedoniya umene unali osauka ukupereka mphaso zake ngati nsembe kwa Mulungu kuti zikathandidzire kuntchito ya Ambuye. Paulo adati kwa iwo kuti sadapereke chomwe akadakwanitsa kupereka koma kuti anapereka chopambana chimene akanakwanitsa kupereka, izi zikutanthaudza kupereka ngati nsembe kwa Mulungu. Vesi 4 ikuonetsa kuti anthuwa amanvetsetsa kuti Mulungu amawadalitsa pakuwalola iwo kuperekako.

B. vesi 6-7 Paulo amalimbikitsa mpingo wa ku Akolinto kuchita zomwe mpingo wa ku Makedoniya udachita-kupereka inde kupereka ngati nsembe. Izi ndizimene Mulungu akufuna mpingo wa ku Africa kuti udzichita.

C. chaputala 9:5-7 chifukwa chimene Paulo adanenera za mpingo wa ku Makedoniya ndikuthandidza mpingo wa ku Kolinto kupereka mwa ufulu kuti akwaniritse udindo wao (vesi 5). Paulo watipatsa chitsanzo chomwe tiyenera kutsatira pamene tikuchita zopereka zathu. Tipereke ndi mtima onse. Mulungu safuna ndalama zanuzo, koma amakulolani inu kupereka ngati mukuchita izi ndi mtima onse komanso ndi chimwemwe.

D. chaputala 9:15 Paulo akutsintha zokamba kuchoka ku zopereka kupita ku ntchito ya Mulungu maka kudzambiri zomwe Mulungu watipatsa ife. Vesi 15 ikuti watipatsa ife mphatso yovuta kuilongotsola kapena kuinena. Tingamulongotsole bwanji Yesu? Palibe Kanthu kuti ndizochuluka motani zimene mupereka ngati kubwedzera kwa Mulungu, sitingapereke kwa Iye, chinthu chilichonse choyenera chofanana pang'ono ndi zomwe Iye amatipatsa ife. Mphatso yake idzakhala ikuperekabe zabwino kwa ife mpaka muyaya.

E. Malaki 3:10-11 akutiudza kumuyetsa Ambuye pakumupatsa Iye mokhulupirika ngakhale tilibe cholingana ndi Mulungu. Marko 12:42-43.

7. Paulo akuchenjedza anthu pa 2 Akorinto 13:3-3 kuti avomeredze ulamuliro wake ndipo adzachita mwa mphanvu ndi iwo, iye akadzadza. Amafuna kudza kuti adzatsangalale ndi mpingo pokhala muchiyanjano limodzi ngati mpingo, osati chidzudzulo. chidzudzulo champingo chiyenera kuchitika ngati pakufunikira kutero. Ndipo akunena pa 13:9-10 kuti chifukwa chomwe timaperekera chidzudzulo ndikubwedzeretsa ochimwa kuchiyanjano cha mpingo.

A. Paulo adatseka kalatayi pa vesi 11 powapempha anthuwa kutaya kutsiyana kwao ndikugwirira ntchito ya Ambuye pamodzi komanso mwa mtendere.

## AGALATIYA-AEFESO

Galatiya ndi mbali ya ku Turkey, ndipo kalatayi idalembedwa kupita kumipingo ya dera limeneli. Mipingo imeneyi idadzalidwa ndi Paulo pamene amayenda m'maulendo ake ofalitsa Mau a Mulungu. kalatayi ilibe malonje chifukwa Paulo adakhudzika kwambiri ndi ziphunzitso zonyenga zomwe zimadzungulira kumeneko ndipo sanafune malonje koma kuti mwachangu akambe za vutoli. Anthu akuphunzitsidwa ziphunzitso zonama pankhani ya chipulumutso. Anthu akuudzidwa kulandila chipulumutso ndi ntchito zao pambali pa

chikhulupiriro. Ntchito zomwe anthuwa amaudzidwa ndi kukhala monga mwa miyambo ya chiyuda komanso ponvera Malamulo antunduwu.

AGALATIYA

Chaputala 1-2 Paulo akunenapo zokhudzana ndi ulamuliro wake.

1.vesi 1-3 Paulo akunena monveka bwino kuti ulamuliro wake anapatsidwa ndi Mulungu otsati munthu.

2. amatsutsa onse amene amaphunzitsa ziphunzitso zonyenga kwa anthu ndipo amafikanso poti anawatemberera iwo pa vesi 9. Kodi choipa ndi ziphunzitso za bodzazi ndichiyani? Chimawachotsa anthu pamatso pa Yesu. Ziphunzitso zonyenga zimawapanga anthu kutsemphana ndi njira ya kumwamba, ndikutenga njira ya kugahena. Njira yabwino kuthana ndi ziphunzitso za bodza ndi kungodalira Baibulo. osakhulupirira chilichonse chomwe wina akunena, chokhudzana ndi Mulungu kapena chomwe Mulungu akuphunzitsa pokhapokha utawona zophunzitsidwazo kuti zilidi mu Baibulo.

3. Paulo akupitilidza pa vesu 10 kunena chinthu chomwe ndichoyambilira kuzonse. Titsatsamalire kutsangalatsa munthu ndi uthenga wathu, koma choyamba titsangalatse Mulungu. nthawi zonse munthu amene amafuna kutsangalatsa Mulungu, amakwiyitsa wina wake. Chitsankho chathu chikhale kutsangalatsa Mulungu ngakhale titakhala kuti titha kukwiyitsa wina wake. Kulalikira za chuma moyo wathanzi ana ndi zina zotere sidzabwino chifukwa timatsiya munthu pakati pa zonse ndipo Mulungu amakhala kuti waiwalidwa.

4. vesi 11-12 ikutiudza kuti tiphunzitse chomwe Mulungu akufuna ife kuti tiphunzitse. Paulo uthenga wake udachokera kwa Yesu ndipo ife timatenga uthenga kuchokera mu Baibulo.

5. Paulo mu chaputala 2 akutsindika kuti atumwi enawo amavomeredza ulamuliro wakendipo kuti sadafune Tito kuti adulidwe, onani vesi 3. Kukanakhala kuti ndikofunikira otembenuka mtima kuti adulidwe, atumwiwo akadalamulira Tito kuti adulidwe. Lero m'dulidwe sinkhaninso, koma mpingo ina imalalika kuti tibatidzidwe ndi kukhala m'moyo wabwino kuti ntchito zimenezi ndi chikhulupiriro zikatipange kulowa kumwamba.

Chaputala 2:15 mpaka chaputala 4 tikunva za kupulumutsidwa ndi chikhulupiriro.

1.timapulumutsidwa ndi chikhulupiriro basi otsatinso ndi ntchito monga m'mene anenera pa chaputala 2:16. Chaputala cha 3 chili ndi uthenga womwewonso. Nvetserani mfundo ya Paulo pa nkhaniyi

A. chaputala 3:1-5 Paulo adakumbutsa Agalatiya za chipulumutso chawo. Pa vesi 3 akufunsa chifukwa chomwe akufunira kuyenjedzera china pa chipulumutso chomwe chidali kale mwa iwo kudzera mwa chikhulupiriro.

B. mu chaputala 3:6-9 Paulo akuwakumbutsa akhristu achiyuda, kuti Abrahamu adalungamitsidwa ndi chkhulupiriro (Gen15:6). Iyi idali nthawi pamene iye anali atsanadulidwe, komanso Malamulo asadaperekedwa kwa Mose. Uwu ndi umboni kuti munthu amapulumutsidwa ndi chikhulupiriro otsati ndi ntchito monga mdulidwe. Judaiza ndi mkhristu amene anatembenuka pokhala muyuda koma amalakalaka kunverabe Malamulo achiyuda. Pali anthu mumpingo lero amene amafuna kulowetsa miyambo ya kwao mumpingomo. Tiwaletse onse obweretsa maganidzo akuti ntchito zathu zingatipangitse kupedza chipulumutso otsati chikhulupiriro chokha.

C. vesi 10-14 Paulo akuti lamulo ndi temberero, vesi 10 ikuti timatembereredwa ndi lamulo ngati sitinvera Malamulo onse. Tchimo limodzi ndilokwanira kutitsiya ife pansi pa themberero. Vesi 11 ikunena kuti timalungamitsidwa ndi chikhulupiriro chifukwa palibe ndi m'modzi yemwe amene adzalungamitsidwe ndi lamulo.

2. ngiti lamulo silipulumutsa nanga ndichifukwa ninji Mulungu anatipatsa ife lamulo?Paulo akuyankha funso limeneli muchaputala cha 3:19-4:7.

A. vesi 19 cholinga chalamulo ndikutidzindikiritsa tchimokotero anthu amadziwa chomwe Mulungu akuyembekedza kuti iwo achite. Onani Aroma 4:15 ndi vesi yonveka bwino.

B. cholinga china cha lamulo ndikuthandidza anthu kuona kutsowekera kwao kotero kuti anthu akatule chikhulupiriro chao pa Yesu yekha.

C. tikuona muvesi 24-26 kuti lamulo limakhala ngati otiyang'anira, pamene tinali pansi pa lamulo. Koma tsopano m'malo mwa lamulo ngati otiyang'anira lero tili ndi chisomo, kotero sitifunanso wotiyang'anira wakaleyu. Lamulo limatumikira zolingazambilri.

i. limakhala ngati mlonda wathu kutitetedza ife kuti tisagwe muchoipa.

ii. lamulo limatitsogorera ife kwa Khristuchifukwa limationetsa kufunikira kwa chipulumutso kwa ife, chifukwa munthu sangatsunge lamulo mwa ngwiro.

D.Chaputala 4:5-7 Paulo akumanga ganizo (onani Aroma 8:15)kuti ife akhristu timatengedwa ngati ana ndi Mulungu. tikuona apa kuti ubale wathu wasintha ndipo kuti tili ndi ubale wopatulika ndi Mulungu. Ndi ife banja limodzi.

3. chaputala 5:1 ndi Aroma 6 zikutiphunzitsa kuti chifukwa tili ndi Khristu tisakhalenso mugoli la uchimo. M'malo mwake tili ndi ufulu kukhala monga m'mene mkhristu amakhalira. Tili ndi ufulu oyenda ndi Mzimu, ndikutsankha kuchita chabwino otsati choipa. Paulo akuphunzitsa chomwechi mu Akolose 3:5-17.

A. akutiudza kuti titsayende mwa thupi. Akunena zinthu zomwe tsitiyenera kudzichitamu vesi 16-21. Machimo omwe Paulo akuwatchula amakwiyitsa Mzimu Woyera ndipo iwo akuchita izi sadzalowa ufumu wa Mulungu.

B. Paulo kenako akutiudza zomwe tiyenera kuchita. Tiyenera kuchta izi zomwe zili zipatso za Mzimu (onani vesi 22-23). Zipatso za mzimu ndi ; chikondi, chimwemwe, mtendere, kufatsa, chilungamo, ubwino, kukhulupirika, ulemu, kudzigwira.

Chaputala cha 6 akulongotsola chaputala 1-10 za zoyenera anthu omwe ali mu uzimu.

2. chaputala 6:1 kuthandidza kubwedza m'bale wosochera.

3. vesi 2 ikuti tithandidzane wina ndi nzache. Njira imodzi yochitira izi ndi popemphererana wina ndi nzache.

4. vesi 3 munthu wa uzimu sanyada.

5. vesi 4 amadzifufudza yekha ndi utumikiwake wa chikhristu kwa Mulungu. khumbo lake limakhala ulemerero wa Mulungu otsati kutamidwa ndi anthu.

6. vesi 5 ikuti munthu wauzimu amakhala ndi udindo woona momwe waimira muuzimu pamaso pa Mulungu.

7. vesi 6 ikuti oyenda mwa uzimu amathandidza aphunzitsi ake pankhani za chuma.

8. vesi 9-10 akuphatikidza zonse pamodzi. Tiyenera kuchita zinthu zabwino ndipo tikangamire kuchita zotere otsalekedza. Vesi 10 ikutipatsa lamulo pothandidza anthu ena. Choyamba timathandidza akhristu anzathu kenako anthu enawo.

## AEFESO

Paulo adalemba kalatayi ali kundende kudziko la Aroma. Sadalembe kalatayi chifukwa chavuto mumpingo, koma chifukwa amafuna kuphunzitsa ziphunzitso za Baibulo. Aefeso ndi mbali imodzi yomwe ikudziwika lero ndi dzina la Turkey, dziko la chisilamu, ku Asiya. Timaphunzira mu vesi 1 kuti Paulo ndi mtumwi ndipo akulembera kalatayi kwa akhristu.

1.chaputala 1:3-14 muchilankhulo chachigiliki, ndi chiganidzo chachikulu chomwe Paulo adalemekedzera Mulungu. vesi 3-5 akuyamika Mulungu Atate maka chifukwa cha dalitso la uzimu limene tinalilandila kuchokera kwa Khristu.

A. Vesi 4-5 akutiphunzitsa kuti Mulungu adasankha anthu ake nthawi zotsayamba asadalenge dziko lapansi. Adapanga izi mwachifuniro cha Iye mwini ndi zolinga zake. Tikuona kuti adatitsankha ife ndi mwa chikondi chake.

2. mu vesi 7-11 Paulo akupereka mayamiko ake kwa Atate kudzera mwa Yesu. Komanso vesi 7-8 tikuona kunti chipulumutso chathu sichichitika malinga ndi ntchito zathu koma chifukwa cha mwazi wa Yesu. Akunena apa kuti ndife okhululukidwa chifukwa cha mwazi wake wokhetsedwawo. Tikuonamfundo iyi kawirikawiri kuonetsa kuti ndi mfundo yofunika kuti tidzinva kuti sitingathandidze Mulungu ndi ntchito zathu kuti tipulumutsidwe. Timapulumutsidwa ndi mphanso ya ulere ya msembe yake otsati kena kali konse ayi.

3. mu vesi 12-14 Paulo kenako akuyamika Mzimu Woyera pantchito yake yotitsindikidza-kutsimikidza kuti tili a kwa Mulungu.

4. vesi 17-18 tikuona kuti ndi Mulungu mwini wake amene amaulula chili chonse tingadziwe chokhudza Iye. Tikuyenera tiwerenge Baibulo lathu mokhulupirika, kulidzukuta ilo ndikufunsa Mulungu, mumphanvu ya Mzimu Woyera, kutiululira zoonadi za Baibulo. zifukwa zomwe mpingo wa ku Africa ungaone kufunika kukhala wofalitsa wa uthenga wabwino ndi kukula muchikristu ndiko kuti chili chonse timafuna chili mBaibulo lomwe tili nalo. Sikufunikira makoleji a Baibulo komanso masemina aBaibulo kubwera kudzalalika uthenga, chachikulu chomwe chilipo ndi Baibulo komanso kulimbikira. Tipemphe kwa Mulungu kudalitsa mphanvu zathu ndikutidzadza ndi mzeru zake. Kumbukirani, chomwe mpingo woyamba unalinacho ndi uthenga wabwino, ndipo Chipangano Chatsopano chinali chikulembedwa chitsanamalidzidwe.

5. chaputala 2:1-10 tikuona akhristu akufotokodzeredwa. Tikuona kuti tinali tonse akufa pamene tinatsata Satana ngati msogoleri wathu. Vesi 3 ikuti tinali anthu ankwiyo wa Mulungu. tinali kupita kugahena, koma vesi 4-5 ikuti chifukwa cha chikondi chake kwa ife adatilanditsa ife ndikutipatsa moyo mu uzimu. Inde monga vesi 6 ikunena, tinakwedzedwa ndi kumwamba ndi Yesu.

A. tikuonanso vesi 8-9 m'mene tinapulumutsidwira. Mwapaderadera tinapulumutsidwa mwa chisomootsati ndi ntchito zathu. Chisomo ndi mphaso yaulere ya Mulungu kwa ife imene ife siitiyenera monga cilpulumutso komanso ngakhale mpweya womwe tikupumawu.

B. vesi 10 ikutiudza kuti sitinapulumutsidwe ndi chifuniro chathu, koma kuti tapulumutsidwa ndicholinga choti tigwire ntchito za bwino. Monga ncthito zabwino sidzingatipulumutse ife, tikudziwa kuti tapulumutsidwa ndi chisomo cha Mulungu kuti tikachite ntchito zabwino. Chisomo cha Mulungu ndukukondera komwe Mulungu amapereka kwa ife chimene ife sichitiyenera ayi.

C. mkhristu amadziwa nthawi yomwe adzamwalire. Kodi mumadziwa nthawi yomwe mudzamwalire? Yankho ndi lokhweka ndipamene mudzamalidze ntchito yomwe Mulungu wakupatsani kuti muchite.

6. chaputala 2:11-22 akhristu tonse ndife olumukidzidwa chifukwa tili amodzi ndi Khristu. Vesi 19 ikutiudza kuti ndife ziwalo za m'nyumba ya Mulungu. khaya ndi iwe muyuda, mu America,mu Africa, mu asia kapena ndani,ngati ndiwe mkhristu ndife ana anyumba imodzi. Munthu wa ku Africa ndi mbale kwa Mbiri ndi munthu wa ku America ngati onsewa ndi akhristu kutsiyana ndi ubale wake ndi mayi wake wotsapulumutsidwa.

Chaputala 4:1-9 tikunva za momwe mpingo ungagwirire ntchito zake.

1.Chaputala 4:11-16 Paulo akupempha umodzi mumpingo. Paulo akuti Mulungu adayitana anthu ku ntchito dzotsiyana mu mpingo kuti amangiridze mpingowo. Tithandidze anthu ena kukula kuti mpingo wonse ukagwirire ntchito pamodzi, kumangirirana wina ndi nzache. Ntchito yathu ngati atsogoleri ndikuthandidza oyera mtima kugwirira ntchito limodzi, kotero tingatumikire Mulungu bwino komanso tingamangirirane bwino wina ndi nzache.

A. chaputala 4:17-32 akhristu titsakhale monga likhalira dziko lapansi. Mwachitsanzo,tionetsa "zipatso za Mzimu" (Agal.5:22-23) m'makhalidwe athu onse.

i. vesi 25 ikutiudza kuti titsamaname koma kunena zoona zokha basi.

ii. vesi 28 ikutiudza kuti tidzigwira ntchito m'malo mwa kuba. Tidzipereka m'malo mokuba.

iii.zoyankhula zathu vesi 29 zimange ubale pa anthu otsati zibalalitse anthu. Yakobo 3:5-10 akutiphunzitsa kuti lilime ndi chida choopsa kwambiri.

iv.vesi 30 ikutiudza kuti titsanvetse chisoni mzimu woyera amene akhala mwa ife. Timachita izi pamene tichimwa mwadala.

v.vesi 32 ikutiudza kutsata zitsanzo za Yesu ndikukhala mu chilungamo kwa wina ndi nzache, ndikuchita changu pokhululukira anzathu. Chikhululuko ndi maki otipanga ife kukhala muumodzi ndi anzathu. Timatha kuchita zinthu zimene zimatha kukwiyitsa anzathu. Ngati ndife achangu pokhululuka tidzamanga ubale wabwino. Banja ndichitsanzo cha bwino. Banja labwino, lodzala ndi chikondi limadzalanso ndi kukhululukirana.

2. chaputala 5 pali malangidzo m'mene tingakhalire ngati akhristu.

A. vesi1-2 ikutiudza kutengera chikhalidwe cha Yesu; monga tanena kale tikhale ngati Yesu.

B. titsamachite nawo zinthu za uchimo za dziko lapansi, makamaka chiwerewere (vesi 3). Vesi 8 monga ikunenera tinali kale ana amumdima, koma tsopano ndife ana a kuunika. Aroma 6 akutiudza kuti sitilinso akapolo a tchimo.

C. vesi 18 ikuti titsakhale oredzera. Palibe chifukwa chokhalira zidakwa chifukwa tili ndi tadzadzidwa ndi Mzimu umene umatilora ife kuonetsa chimwemwe, kuthokodza, ndi kudzipereka.

D. mbali yotsilidza ya chaputalachi ikunena za ubale wa pakati pa mkazi ndi mwamuna wake. Ili ndi phunziro lofunikira kwambiri. Zina mwa ziphunzitsozi zimasiyana ndi zochitika zathu, koma apa Mulungu akutipatsa ndondomeko ya banja la bwino, lomwe limalemekedza Mulungu. Mulungu amakonda mkhristu wa mkazi m'mene amakondera mkhristu wa mwamuna.

E. tione malangidzo a Mulungu pa mabanja athu.

i. vesi 22-24 ndimalangidzo kwa adzimayi pa dzautsogoreri wa mbanja. Mwamuna ndi mtsogoleri ndipo amatenga udindo wonse wa mbanjamo. Mzimayi agonjere ku ziganidzo zonse ndi chilemekedzo. Izi zikutsekula phunziro lofunikira kwambiri lomwe likubwera patsogolopa.

ii. vesi 25-33 ikupereka kwa mwamuna maudindo ake oyenerera.

iii.vesi 25 akuphunzitsa amuna kuti akonde akazi awo ndi chikondi chomwe Khristu adali nacho ndi mpingo wake. Kodi yesu adaukonda mpingo wake kwakukulu bwanji? Iye adaufera iwo, azibambonso adzilolera kufera akazi wawo.

iv.cholinga cha chikondi chathu ndi monga vesi 26-27 ikunenera, kumumangirira mkaziyo mwa Ambuye. Ife azibambo tiyenera kukhala atsogoleri a uzimu.

F.kumathero konse kwa chaputalachi tikunva kuti m'maso mwa Mulungu tili thupi limodzi ndi akazi athu. Choncho ife azibambo tizichita ndi akazi athu, monga ife timafuna kuti ena azitichitira.

3. Chaputala 6:1-4 akuyamba kuphunzitsa za ubale wa pakati pa ana ndi makkolo awo.

A. ana anvere makolo awo, ili ndi lamulo lachitsanu.

B. Makolonso apa ali ndi udindo. Tilele ana athu ndi ganizo lakuti iwo ndi ofunikira. Kumbukirani 2 Akor. 2:4 pamene akuti makolo ali ndi udindo kwa ana awo. Ife makolo tiphunzitse ana athu zokhudzana ndi Mulungu. nkhaniyi ndi yofunikira kwambiri. Rpamene vesi 4 ikunena kuti tiyenera kuzuzula ana athu tinvetsetse kuti kumenya sikuzuzula mwana ayi. Cholinga cha chuzuzulo kwa mwana ndi kumudzindikiritsa cholakwitsa chomwe wachichita ndikumuphunzitsa kuchita chomwe chili choyenera. M'menyeni mwana pomuphunzitsa koma otsamenya mwana mutakwiya/kupsa mtima.

4. vesi 5-9 ikunena za ubale wa akapolo ndi ambuye awo uwu unali ubale munthawi ya Baibulo. lero nkhaniyi ili pakati pa antchito ndi mabwana awo. Akapolo kapenanso anthu olembedwa ntchito akuyenera kukhulupirika ndi ulemu pa ntchito kwa abwana awo. Komanso mabwana achite ndi antchito awo mofanana ndi momwe ambuye wa akhristu Yesu amachitira ndi ife. Malaki 3:5 pali malangidzo kwa olemba ntchito pamene anamidza omugwirira ntchito. Kuli mawu ku America kuti; "malipiro oyenera patsiku amaperekedwa pa ntchito yoyenera.

5. phunziro lotsilidza mu chaputala chimenechi likuyamba pa p vesi 10-18.

A. tidziwe kuti tili pankhondo ya mu uzimu ndi njerekedzi ndipo kuti Satanayo ndi wamphanvu kupotsa ife. Onani Yuda vesi 9 kuti ngakhale angelo amphanvu, wamkulu wa

angelo Mikaelo sanalimbane ndi Satana moonekera. Tilimbane ndi Satana pogwiritsa ntchito zida za Mulungu chifukwa sitilimbana ndi anthu koma mdani wathu demoniyo. Pemphero ndi chida chathu cha mphanvu.

6. Paulo akupempha pa vesi 19 kuti mpingo wa ku Aefeso umupemphere iye. Atsogoleri anse a chikhristu amatsowekera kupemphereredwa.

## AFILIPI-AKOLOSE

Paulo ali kundende pamene akulemba kalata imeneyi kumpingo wa ku Filipi kumpoto kwa Gilisi. Amafuna kuwadziwitsa iwo za moyo wake ndi kuwathokodza pa mphaso zomwe adatumidza. Alinso ndi maphunziro kupita kwa iwo okhudzana ntchito komanso kuipa kwa ziphunzitso zonama.

### AFILIPI

1.kalatayi adalembera akhristu a ku Afilipi.

2. nfundo yaikulu ya chaputala 1:1-19 ndiyakuti pokhala kundende tsidzinatsokonedze utumiki wa Paulo. Adagwiritsa ntchito mwayi amakhala nawo kulemba mabuku ena a Chipangano Chatsopanokomanso kulalikira uthenga kwa anthu ambiri kuphatikidzapo akaidi anzake. Paulo tsanataye mtima koma ngakhale kundende adapitilidzabe kugawa uthenga wabwino.

3. Paulo akulongotsola kuti tsakuopa imfa. Amadziwa kuti atha kuphedwa nthawi iliyonse, koma kuti adayankhula pa vesi 21 zito mkhristu kufa ndi kupindula. Atha kutaya moyo wake pansi pano koma amakapedza wina kumwamba.

4. mu vesi 20-26 pamene wapanidwa ndi kukhala ndi moyo komanso kufa, iye akufuna atakhala ndi moyo chifukwa pakutero adzathandidza mpingo kopambana. Cholinga chathu kukhale kutumikira Mulungu ngakhale izi zitakhala kuti zikhodza kuika moyo wathu mu msauko, komanso otsakhudzika kwambiri ndi imfa yanu chifukwa pakufa sitingaluze Kanthu. Tonse tidzikhala ofunitsitsa kutero. Monga vesi 29 ikunenera, tivutike pachifukwa cha uthenga wabwino.

5. chaputala 2 Paulo akudzindikila kuti anthu a ku Afilipi adali okhudzidwa ndi moyo wake. Choncho adawaudza iwo kukhala mu umodzi. Izi zingachitike ngati akuganidza monga Yesu (vesi 5). Mulungu akhale chinthu cholingalilapo kopotsa; Mulungu akhale zonse mu zonse.

6. chaputala 2:9-11 ikunena china chake chomwe ndi nfundo kwa akhristu komanso mkhamba kamwa kwa achikunja. Aliyense avomeredze kuti Yesu ndi Mulungu. Ife akhristu tichite izi ndi mtima wa chitsangalalo. Munthu wotayika amachita ichi ndi mtima wokayika, pa chiwerudzo chake pamene akadali munjira ya kugahena.

7. chaputala cha 3 Paulo akuchenjedzanso za aphunzitsi onyenga mu mpingo.

A. Paulo akunena pa 3:3-11 kuti samagwiritsa ntchito chikhulupiriro kuti akhale otsatila wa lamulo. Iye amachita izi kuti adzipedzere yekha chipulumutso. Akuti kukanakhala kotheka munthu kudzipedzera yekha chipulumutso, mwachidziwikire iye akadachipedza. Mu vesi 7 iye adapedza kuti kuyetsa kwake kunalibe kanthu pachipulumutso. Akudzindikira tsopano kuti (vesi 9) chilungamo chake chimachokera mu chikhulupiriro pa Yesu Khristu.

B. mu vesi 12-21 Paulo akuti tigwire ntchito maka pokwaniritsa cholinga chofuna kutumikira Yesu ndikukhala ofanana ndi Iye. Akunena mu vesi 20 kuti kwathu kwenikweni ndi

kumwamba, ndipo tikudikira Yesu amene adzatsinthe matupi athu ofokawa kuti adzakhale a ulemerero.

8. Paulo mu 4:1 akuonetsa mtima woona wa mbusa. Amakonda anthu ake ndipo amafuna kukhala ndi iwo. Chidzindikiro choona cha mbusa sikukhala odziwa kuyankhula koma kukonda ndi kutsamala anthu ake. Amawatsamala kuthupi ndi ku uzimu, monga Yesu adatumikira anthu komanso iye ndi mbusa wabwino.

9. mu vesi 2-3 Paulo akunena za anthu awiri amene akhala amakangana, ndipo wa apempha iwo kuti aleke kutero. Adapempha anthu ena mumpingomo kukhala ankhala pakati ndi kuthandidza Euodiyo ndi Suntuke kuti aleke kukangana ndi kugwira ntchito limodzi mu mpingomo.

10. tikufunikira tonsefe mtima wa Paulo. chaputala 4:10-13 tikunva kuti palibe Kanthu kuti ndi ife otsauka motani, koma tikhale okwanitsidwa ndi zomwe tilinazo. Ngati mulungu watipatsa ntchito yovuta, kapena yoopsa tikuyenerabe kukhala okhutitsidwa.

A. onani chilimbikitso mu vesi 19 pamene Mulungu akunena kuti adzatipatsa chili chonse chomwe tichifunadi. Otsati chomwe tikuganidza koma chomwe Mulungu akuchidziwa kuti zoonadi ndi chofunika. Kumbukirani kuti ngakhale nyengo zathu zitilodzera kuimfa komabe tidzakhala opambana, onani 2Akor. 5:8. Mkhristu nthawi zonse amakhala opambana.

## AKOLOSE

Paulo adalemba bukuli kupita ku mpingo wa Akolose komwe adali atsanafikeko. Adalemba bukuli ali kundende. Adalemba ndicholinga chotsutsa chiphunzitso chabodza chomwe chinabuka mu mpingomo. Tikuonanso kuti mchitidwe wa Atuda ukubweretsanso vuto mu mpingo. Iwo molakwitsa amatsimikidza kuti Yesu yekha sangapangitse munthu kupulumuka. Paulo adalemba kalatayi pofuna kukonza mavutowa.

1.Paulo akuyamba ndi kulonjera mpingowo ndikukumbutsa anthu kuti iye adatsankhidwa ndi Mulungu kuti akhale mtumwi, ndipo ulamuliro wake umachokera kwa Mulungu.

2. ngakhala Paulo akulemba bukuli pokonza mavuto omwe adali mumpingomu, sakungoyamba ndi kunena za vutolo. M'malo mwake mu vesi 8 akuyamba kunena za zinthu zabwino zomwe adaphunzira. Iyi ndi njira yabwino yokopera munthu kuti akhale mbali yako, koma ngati ungoyamba zonena zako potsutsa zikhulupiriro za anthu ena anthuwo amatetedza mbali yawo ndipo pakutero samanvera zomwe iwe ukunena. Njira yabwino yokopera munthu ndi kungomuudza njira yoyenera kuchitira zinthu ndipo kumutsiya kuti aone vuto lake pamene akunvetsera zonena zako otsamuudza iye kuti ndi olakwitsa.

A. zinthu zabwino zomwe adaziphunzira ndi chikhulupiriro ndi chikondi vesi 4 komanso chiyembekezo mu vesi 5.

3. Paulo pa vesi ya 13-19 tikuphunzirapo za Yesu.

A. vesi 13-14 akuti Iye ndi muomboli wathu.

B. chaputala cha 1:15 akuti ndi olowa m'malo a kulamulira zolengedwa zonse za padziko lonse.

C. Yesu ndi mulengi wa zinthu zonse vesi 16-19 ndipo ndi Iye woyambirira wa zinthu zonse. Ndi mutu wa mpingo.

4. vesi 20-23 akutiphunzitsaso kuti Yesu ndi chiyembekedzo cha dziko lapansi.

5. tikuona pa vesi 1:24-2:3 kuti Woyera wina aliyense (vesi 26) wapasidwa chinsisi kuchokera kwa Mulungu amene ali Yesu Khristu. Timapedza mayankho athu kuchokera mu Baibulo

6. Paulo kenako mu chaputala cha 2:4-8 akuwaudza iwo kuti cholinga cha chiphunzitso chake ndi kuwatetedza iwo ku ziphunzitso zonama, zomwe zingawasocheretse ndi kuwapanga kuti asakhale akhristu.

7. chifukwa cha Khristu, vesi 9-23 tikuphunzira kuti palibe chifukwa chotsatila malamulo a chikhalidwe monga ngati kuletsa zakudya kapena mdulidwe pofuna chipulumutso.

A. vesi 11-13 mwa khristu ndi tinapatsidwa mdulidwe otsachitika ndi manja (Akolose 2:11) pa ntchito ya kubadwa mwa tsopano mwa ife, umene uli mdulidwe wa uzimu kwa akhristu. Ndi muyuda wa mkati, ndipo mdulidwe wake ndi wamuntima (Aroma 2:29). Ichi ndi chochokera kwa Khristu kupita kwa akhristu padziko lonse lapansi. Ndi chinthu chotsachitika ndi manja; otsatinso ndi mphanvu ya cholengedwa chilichonse koma ndi mphanvu ya Mzimu wodalitsika wa Mulungu.

8. potero kuti tinaukitsidwa ndi Khristu, 3:1-17 kotero tifunefune zinthu zakumwamba. Monga Agalatiya pamene tmaona za zipatso za Mzimu, Paulo akutiudzanso chomwe tingachite ndichomwe sitiyenera kuchita.

A. chaputala 3:5-9 pali ndandanda wa zinthu zomwe tiyenera kuchita, chifukwa tinavula munthu wakale ndipo ndi ife zolengedwa zatsopano.

B. tiyenera pa vesi 10-11 tivale munthu watsopano ndipo tikuudzidwa kukhala ndi makhalidwe onga a Yesu.

C. vesi 17 ndi imodzi mwa mavesi akuluakulu ofunika kulowedza. Zonse zomwe tichita zichitika mudzina la Ambuye. Tichite chilichonse ndi chiyamiko komanso ndi ulemerero kwa Mulungu. Ngakhale m'mavuto tichite zonse kuulemerero wa Mulungu, onani Yakobo 1:2. Pamene tilima m'munda mwathu, tichite izi ndi chiyamiko cha m'mitima mwathu.

9. chaputala 3:18-22 Paulo akupereka malangidzo okhudzana ndi makhalidwe a mbanja la chikhristu. Agwiritse ntchito zonse zomwe aphunzira za chikhristu pa banja lawo.

10. chaputala 4:2-6 pali malamulo anayi kuti atsatidwe ndi membala wina aliyense wa mumpingo.

A. choyamba atsaleke kupemphera. Vesi 2-3.

B. akhale oyamika mu zonse. Vesi 2

C. ayenda mu nzeru pakati pa otsakhulupirira. Vesi 5 Paulo akuwalangidza kukhala achilungamo kwa anthu akunja, pakutero mudzawakopera iwo kwa Khristu.

D. chotsilidza, zoyankhula zathu zikutidwe ndi chisomo. Vesi 5-6.

11. Paulo akutsilidza kalatayi powadziwitsa anthuwa za Tukiko amene adzamuyimirire Paulo kulimbikitsa mpingo. Chaputala 4:7-8.

12. Paulo pa vesi 15 akutchula za mpingo wa m'nyumba. Malo ambiri padziko lapansi akhristu ambiri amakumana mumipingo ya m'nyumba. Kwenikweni izi zimachitika kumaiko

komwe akhristu amazunzidwa kwambiri. Sikololedwa m'maiko a China, ndi Saudi Arabia kuti akhristu azikumana pokapokhamo muli mwa chinsinsi muzinyumba.

## ATESALONIKA

Makalata awiriwa Paulo adalembera kumpingo wa kwa Atesalonika umene uli ku mpoto kwa Gilisi. Paulo adagwiritsa ntchito makalatawa pophunzitsa zinthu zochulukirapo.limodzi mwa phunziro la makalatawa ndi zokhudzana ndi matsiku otsilidza, ndiponso adagwiritsa ntchito makalatawa pothandidza kulimbikitsa mpingokupirira pa nthawi ya ntsautso.

Paulo akuyamba kalatayi polimbikitsa anthu. Adali akudzunzidwa kotero Paulo adawalimbikitsa iwo. Ichi ndi chinthu chabwino kuti atsogoleri ampingo adzichititа kwa anthu awo. Ndi udindo wathu kulimbikitsa mamembala athu ndikuwathandidza pa nthawi ya ntsautso.

1.adayamba muchaputala cha 4 kunena za mavuto ena amumpingo. Onani vesi 1 pamene Paulo amanena kwa Akhristu kuti tidzikhala m'moyo wokondweretsa Mulungu. ichi ndi cholinga cha mkhristu nthawi zonse. Paulo pa vesi 2 akuwaudza anthu kuti ayenera kunveredwa chifukwa ulamuliro wake umachokera kwa Mulungu.

2. Vesi 3-8 ikunena za chiwerewere. Ili ndi vuto lalikulu kwa akhristu monga tikuona kuti mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano akutiphinzitsa kukhala otsamala ndi otsadetsedwa ndi nkhani za chiwerewere. Akulu ampingo ambiri agwa chifukwa cha nkhani za chiwerewere. Tipewe kuti tisagwe mu tchimo la chiwerewere. Njira yabwino yodzitetedzera ndi pemphero komanso otsakhala m'malo momwe timadziwa kuti titha kugwa mkuyetsedwa. Chitsanzo cha izi ndi kutsayendera munthu olekana ziwalo uli wekha. Nthawi zonse mudzikhala ndi munthu wapadera ngati mboni yanu patagwa zinthu zina.

A. kumaiko a azungu azibusa ambiri ndi ophunzira ubusa agwa chifukwa choonera zinthu zolaula pamene akugwiritsa ntchito intaneti.

B. chilakolako cha chiwerewere ndi choopsa kwambiri mwa ichi tidzitetedze tokha pamene pakufunikira kutero, monga Aefeso 6 akuphunzitsira kuti tivale zida zonse za Mulungu. kumbukirani monga Paulo anenera mu chaputala cha 4:5 tisakhale ngati otsakhulupirira amene satha kudziletsa okha. Paulo akutiphunzitsa za m'mbuyo pa Aroma 6 kuti si ifenso akapolo a tchimo. Kotero tidziretse kuti titsagwe mu mayetsero a chiwerewere.

C. Paulo mu vesi 8 akunena kuti timaonetsa kutsanvera Mulungu pamene tikhala mum'chitidwe wa chiwerewere, koma titsagwe ku tchimo limeneri popedza Mzimu Woyera akhala mwa ife kutithandidza kupewa tchimo, ndipo ndi thandizo la Mulungu tidzakwanitsa kugonjetsa ntchimo.

3. Paulo mu vesi 9-12 ali ndi ziwiri zoti atiphinzitse.

A. choyamba Paulo adawaudza iwo kuti akuchita ntchito yabwino pothandidzana wina ndi nzache, poonetsa chikondi cha umodzi. Amawalimbikitsa apa kuti apititlidze zimenezi.

B. mwachidziwikire, chaputala 4:11-12 anthu ena samagwira ntchito kuti adzipedzere okha zofunikira pa moyo wawo watsiku ndi tsiku. Kotero Paulo amawadziwitsa kuti tikuyenera kugwira ntchito kuti tidzithandidze tokha otsati kukhala chipsinjo kwa anzathu. Chomwe chimachitika kumpingowu ndi chakuti anthu amayembekedzera kuti Yesu abwera potsachedwa kotero adatsiya kugwira ntchito. Palibe akudziwa tsiku lomwe Yesu adzabwere, kotero tikhale m'moyo woyenera pamene tikumuyembekedza iye.

4. Paulo pa vesi 13-18 akuwatsimikidzira anthuwa kuti Yesu adzabweranso choncho adawaphunzitsa zomwe zidzachitike pamene Yesu akubwera kachiwiri;

A. vesi 16 ikutiudza kuti okufa choyamba adzadzuka.

B. vesi 17 ikutiudza kuti kenako anthu onse ati adzakhale ndi moyo adzatsatira kukkumana ndi Yesu mlenga lenga ndipo tidzakhala ndi Yesu kwa muyaya. Ndi chilimbikitso chachikulu kwa ife kuti pamene mkhristu nzathu yemwe timamukonda wamwalira tidzakumana naye kumwamba. Pali mau amati “akhristu asamati basi tapita koma adziti tidzaonana nthawi ina.”

5. chaputala 5:1-2 tikunva kuti Tsiku la Ambuye likubwera. Kodi Tsiku la Ambuye ndi chiyani?

A. Mauwa adayamba kugwiritsidwa ntchito mu buku la Yesaya 13:6 pakuti tsiku la Ambuye layandikiramonga chipatsula cha Ambuye chidza ndi Tsikuli; Mauwa atchulidwa maulendo okwana 23 mBaibulo, ku Chipangano Chatsopano ndi Chakale chomwe. Onaninso Yoweri kuti muone tanthauzo la mau oti Tsiku la Ambuye, pa chiwerudzo cha ana a Israeli. Ndi nthawi ya chiwerudzo. Werengani Yoweri 2:1-11 kuti muona kuopsa kwa Tsiku la Ambuye maka pa chiweruzo.

i. tsiku la Ambuye litha kutanthaudza nthawi yomwe tikukhala padzko la pansi. Ndi nthawi ya chiwerudzo choopsa chifukwa cha tchimo. Moyo m’maiko ambirimbiri umaonetsa kuti tikuzunzika chifukwa cha machimo athu ndipo kwa anthu otere ili ndi tsiku la Ambuye. Mwachitsanzo, mazunzo ambiri padziko la pansi akuyambitsidwa ndi maboma otsaopa Mulungu lomwe ndi vuto la tchimo.

ii. mwachizolowedzi tsiku la Ambuye limatanthaudza kubwera kwa Yesu kachiwiri kudzawerudza dziko anthu onse; nthawi yotsilidza. Kwa anthu ambiri tsikuli lidzakhala la chiwerudzo chowawa kwambiri.

iii.tsiku la Ambuye ndi tsiku lomwe akhristu adzalandire mphoto ya moyo wotsatha.tikambe kutsiyana kwa moyo wa akhristu ndi achikunja pa tsiku la Ambuye. Akhristu adzakhala akuyan’gana tsikuli chifukwa ndi tsiku lomwe tidzalandiridwe kumwamba ndi Yesu. Anthu achikunja monga tanena kale adzayamba ulendo wa chilango chotsatha ku Gahena.

B. Paulo mu chaputala 5:1-11 akutitsimikidzira ife akhristu kuti titsaope pa tsiku la Ambuye. Akuchita izi poonetsa zochitika zotsiyana pakati pa akhristu ndi anthu achikunja. Tiyeni tione zitsanzo zochepa chabe;

i. vesi 5 ikutitsimikidzira kuti ndi ife ana akuunika otsati mdima.

ii. vesi 9 ikutitsimikidzira kuti sitinaikidwe kuti tikaonongeke.

iii.vesi ikutitsimikidzira kuti tidzakhala ndi Yesu khaya tamwalira kapena tili ndi moyo.

C. chaputala 5:12-22 akutipatsa ife malangidzo otsilidza.

i. vesi 12 ndi 13 tikuphunzira kulemekedza onse omwe ali ndi udindo komanso ogwira nawo ntchito limodzi ku mpingo.

ii. vesi 14 ikulangidza akhristu olimba kukulimbikitsa akhristu ofoka omwe tsakuchita chomwe adayenera kuti achite.

B. vesi 15 tikuphunzira kuchitira zabwino onse amene akutichitira mwano. Kumbukirani zonwe Yesu adanena pa chiphunzitso cha paphiri, onani Mat. 5:39 komanso Miyambo 25:22 ndi Aroma 12:20.

7. Paulo mu vesi 16-22 akutipatsa malamulo otsiyanatsiyana.

A. vesi 16 kondwerani nthawi zonse.

B. vesi 17 pempherani kotsalekedzatidzikhala ndi ndondomeko ya kapempheredwe nthawi zonse. Tikhale nthawi zonse ndi ntima wa pemphero. Otsakhala kutali ndi pemphero.

C. vesi 18 yamikani muzonse. Izi nthawi zina zimakhala zovuta, koma kumbukirani kuti palibe kanthu nyengo yanu ndi yotani, palibe angalande inu chimwemwe cha chikhristu chanu. Nthawi zonse tiyang'ane kumwamba ndikupangitsa mtima watha kukhala oyamika muzonse.

D. vesi 19 ikuti titsazime Mzimuyo; timachita izi pamene tiyenda munjira ya Satana, ndikunyodzera Mau a Mulungu.

E. vesi 20 mutsanyodzere manenero-tilandire chiphunzitso chochokera m'mau a Mulungu.

F. vesi 21 yetsani zonse- yetserani zonse ndi Mau a Mulungu. tiphunzire Baibulo ndipo pamene wina aphunzitsa china chake chkhudzana ndi Mulungu, tionetsetse kuti chikuvomeredza zonena za mBaibulo. Baibulo ndi mulingo woyenera wa Mulungu.

G. Vesi 21 ikuti gwirani chamwe chili chabwino. Tivomeredze zinthu zomwe zili zabwino pamatso pa Mulungu. tichite zomwe zili zabwino pamaso pa Mulungu.

H. vesi 22 pewani choipa. Kotero tiphunzire chomwe chili chabwino pogwiritsa ntchito Baibulo. pakutero tidzachita chomwe chili chabwinondipo tidzatsankha kutsachita choipa.

8. Paulo akumalidza chiphunzitsochi potiudza ife mu vesi 23 kuti tiyende pamaso pa Mulungu mokhulupirika. Sitiyenera kutsatira woipayo. Vesi 24 ikunena kuti Yesu adzatithandidza kuchita zinthu.

## ATESALONIKA WACHIWIRI (2 ATESALONIKA)

Bukuli lidalembedwa patangotha miyedzi yochepa chilembere kalata yoyamba ija poyankha ena mwa mauthenga amene Paulo adawalandila kuchokera kumipingowu. Uthenga wa Paulo mu kalatayi ndi Masautso, kubweranso kwa Ambuye ndi kufunikira kokhala moyo wa uzimu.

1.Chaputala cha 1:4-12 ikunena za matsautso.

A. Paulo akuwaudza kuti ndiokondwa m'mene iwo akhalira muchoonadi cha Yesu ngakhale ali mu ntsautso. Uwu ndi umboni kuti oti ndi oyenera kukhala akhristu. Vesi 4-5.

B. Amene akupangitsa kuti akhristu azidzunzika iwonso adzazunzidwa ndi kutsautsidwa kwa muyaya. Vesi 6 ndi 8-9.

C. kunzunzika kwathu ndi kwanthawi yochepa. Vesi 7.

D. Paulo akukhumba kuti Mulungu adziremekedzeka pamene tikudzunzika. Vesi 12 nthawi zina munjira yomwe ife sitinvetsetse, Mulungu amakhala kuti akulemekedzka mu ntsautso yathu ndipo ufumu wake umakhala ukupita patsogolo.

2. Chaputala 2:1-12 akunena za mantha amene ena mwa oyera mtima ali nawo. Amaopa kuti atsemphana ndi tsiku la Ambuye; kuti Yesu anabwera kachiwiri kwa anthu ake ndipo kuti iwo atsemphana naye. Paulo akuti ichi sichinachitike chifukwa zizindikiro za kudzakwake sizinaoneke.

A. chimodzi mwa zizindikiro ndi chakuti munthu wosutsana ndi lamulo sanabwere. Uyu ndi munthu yemwe adzakhale ochimwiratu amene adzafune anthu azimupembedza m'malo mwa Mulungu. idzakhala nthawi yakuukira kwakukulu. Vesi 3 mumbiri anthu amati izi zinachitika kale koma ife sitinganene kuti zinachitikadi kapena ayi kuti munthu otsayenda muchilamuloyi ndi ndani.

3. muchaputala cha 3:10-13 Paulo akupempha okhulupirira kuti atsakhale manja lende. Agwire ntchito ndikupedza zofunikira pa moyo wao. Poonetsa kufunikira kwa izi vesi 11 ikuti munthu otsagwira ntchito asadye. Paulo akuti iyi ndi njira yoyimitsira nchitidwe otsagwira ntchito.

A. komanso vesi 13 monga tinaona mu Agalatiya 6:9 tikulimbikitsidwa kugwira ntchito molimbika otsati kugwa mphwayi kutumikira Ambuye. Tikhale otsamala kugwira ntchitotyi kwanthawi yaitali. Akhristu ambiri amayetsera kugwira ntchito kwambiri, ndipo pamapeto amatopa ndikutsiya kugwira ntchito ya ufumu wa kumwamba. Tigwire ntchito molingana ndi muyezo wake kuti titsatope mwachangu koma tigwire ntchitoyo kwa nthawi yaitali.

## TIMOTEO-FILEMONI

Paulo adalemba makalata awiri kwa Timoteo kumulimbikitsa ndi kumulangidza. Timoteo atangotembenuka mtima adakhala mbusa ndipo amakumana ndi nyengo zolimba kwambiri. Paulo adalembera kwa Timoteo ndi Tito pofuna kuwalangidza azibutsa ochepa nsinkhuwa, m'mene angagwirire ntchito mopindulitsa. Adawachenjedza iwo za kuopsa kwa aphunzitsi achinyengo, adawalimbikitsa iwo pamene akumana ndi mazunzo ndipo adawalangidza pamene pankhani ya chipembedzo ndi utumiki.

## TIMOTEO WOYAMBA (1 TIMOTEO)

1.Mbali yoyamba ndiyokhudzana ndi aphunzitsi onyenga chaputala 1:3-11. Akutchula Humenayo ndi Alesandro ngati aphunzitsi awiri onyengamu vesi 20. Pamene Paulo akuti ndawapereka mudzanja la Satana akunena kuti waatulutsa anthu aiwriwa mu mpingo. Tiphunzire izi ndi kuchita momwe tingathere pofuna kulimbana ndi ziphunzitso zonyenga mu mpingo mwathu.

2. Paulo akutsogolera mpingo kukhala ndi moyo wa mapemphero. Akuupempha kuti uzipempherera anthu ena. Chaputala 2:1-2 Paulo akuwatsogorera iwo kupempherera ena monga ngati atsogoleri kotero kuti monga vesi 2 ikunena tidzakhala ndi mtendere ndi moyo wa ulemu.

3. chaputala 2:9-15 pali malangidzo a udindo wa amayi mu mpingo. Adalangidza azimayi kuvala moyenerera mumpingo. Adalamulanso kuti (vesi 12) amayi asakhale ndi ulamuliro kwa abambo.

4. chaputala 3 pali malangizo amomwe mpingo ungayendetseredwe.

A. vesi 1-7 ikunena za udindo umodzi ndi mayina atatu otsiyana koma okhala ndi tanthaudzo limodzi- akulu abishopu komanso abusa. Tikunva kuti waudindoyu akhale mwamuna wa

Mbiri ya bwino. Odziwanso kulamula banja lake. Akhale ndi mkazi m’modzi. Akhalenso odziwa kuphunzitsa Baibulo. akulu a mpingo amalamula mpingo chifukwa cha utsogoleri wa Yesu. Akulu a mpingo akhale zitsanzo ku mpingo.

B. vesi 5 ndi nfundo yakuti munthu amene salamula bwino zinthu zake sangakwanitse kutsogolera mpingo wa Mulungu.

C. Vesi 6 ikunena za nfundo zikuluzikulu. Mutsapereke udindo kwa munthu amene wangokhulupirira kumene. Mudikire panthawi imene akula ndi kuonetsa zizindikiro zokhwima muuzimu.

D. akulu a mpingo ali ndi zochita zambiri, kotero titsamale pamene tikuwasankha. Koyamba ayenera anve kuitana kwa Ambuye. Ndipo kuitanaku kuvomeredzedwe ndi mpingo. Munthu asamangoganidza poyerayera kukhala mbusa kapena mkulu wa mpingo.

5. vesi 8-13 akunena za atumiki amene amachita zinthu zambiri zokhudzana ndi mpingo zooneka ndi maso. Tikuona kuti iwonso ayenera kukhala ndi mbiri yabwino. Ayetsedwe (vesi 10) zomwe zikutanthaudza kuti atsakhale anthu omwe angokhulupirira kumene, ndipo aonetse kuti amakhala monga momwe mulungu afunira.

6. chaputala 3:15 akunena kuti mpingo ndikumene choonadi cha Khristu chilalikidwe ndi kutetedzedwa. Paulo pachiyambi walangidzapo m’mene anthu angakhalire ndi m’mene atsogoleri eyenera kusankhidwira. Chaputalachi chili ndi zinthu zomwe zimachitika ku mipingo.

7. chaputala 4:1-5 ndichenjezo kwa akhristu kutsamala kuti asalolere chiphunzitso chonyenga kulowa mumpingo chifukwa atsogoleri ena samatsatira chiphunzitso cha Baibulo.

8. chaputala 4:6-16 nfundo yoyamba ikupedzeka mu vesi 6 imene ikuphunzitsa kuti mulaliki wabwino ndiyekhayo amene waphunzitsidwa m’mau a chikhulupiriro. Izi zikutanthaudza kuti alaliki akhale ophunzira a Baibulo. Titsaphunzitse kapena kulalikira Baibulo titsanaliwerenge ndi kulinvetsetsa chomwe likuphunzitsa ndi kutanthaudza.

A. vesi 7 ikuti asakhale ndi nthano zomwe zikutanthaudza kuti asaphunzitse chili chonse chomwe sichichokera mu Baibulo. Kumbukirani kuti tsitikhulupirira chilichonse chokhudzana ndi Baibulo pokhapokha titachiwerenga mu Baibulomo, tikubwerezanso kuti tili ndi udindo kuphunzitsa ndi kulalika chokhacho chomwe chili m’Baibulo. Izi ndi zoikika za Mulungu. Ichi ndi chinthu cha chikulu kwambili.

B. vesi 13 ikulangidza za kuwerenga Mau a mulungu pagulu kuti kukhale koyenera. Ndikwabwino mpingo kuwerenga Mau a mu Baibulo mofuula pa tsiku la Ambuye la Mulungu pa nthawi ya chipembedzo.

C. vesi 15-16 mkulu wa mpingo adzichita chomwe akulalikira, otsangolankhula koma otsachita. Tikhale zitsanzo zabwino.

9. Chaputala 5 tikuphunzira za udindo mkati mwa banja.

A. vesi 1-2 ikuphunzitsa mbusa kulemekedza ndi kukonda mamembala a mpingo wake monga m’mene amchitira ndi banja lake.

B. vesi 3-6 akuphunzitsa m’mene mpingo ungachitire ndi azimayi amasiye.

i. pedzani omwe ndi amasiyedi. Awa ndi omwe alibe wina aliyense owathandidza. Ndi udindo wa banja kutsamala amasiye awo. Ngati palibe vesi 16 ikuti mpingo utenge udindowu. Nanga ngati pali banja lomwe silikutsamalira amatsiyewa-kodi mpingo utenge udindowu. Maganizo anga ndiakuti eee! Ndikukhulupirira kuti chiphunzitsochi chiyeneranso kuchita chimodzi modzi ndi ana amasiye (Yakobo 1:27).

ii. vesi 14 ikuphunzitsa kuti ndikwabwino mkazi wa masiye kukwatiwanso kotero ndi kwabwino abambo kukwatiranso amayi amasiye.

10. chiphunzitso china ndi ulangidzi wa mpingo m'mene angachitire ndi abusa komanso akulu a mpingo. 5:17 ayenera kupatsidwa ulemu ndipo vesi 18 ikuti ayenera kulipidwa makamaka abusawo. Mpingo ungalipire mbusa pamene uli ndi ndalama ndipo mipingo yambiri imatsowa ndalama koma ngati angakwanitse mbusa ayenera kulipidwa. Ndikwabwino ngati mpingo kukhala ndi mbusa yemwe angakhale pamenepo nthawi zonse amene angapereke nthawi yake yonse ku ntchito ya ambuye ndiponso otsapita nakagwira ntchito ina kuti pofuna kupedza dzotsowa zake.

A. vesi 19-21 akunena za kutsutsa mbusa kapene mkulu wa mkulu wa mpingo pamene wachita cholakwika. Choyamba ndichakuti otsamuikira iye mulandu popanda mboni. Otsachita miseche yokhudza atsogoleri a mpingo wanu. Nthawi zonse mudzifuna kuthandidzana ndi iwo otsati kutsutsana nawo.

B. komabeAbusandi akulu ampingo awiri onsewa ndi ochimwa ndipo vesi 20 ikunena iwowa ayenera kupatsidwa chidzuzulo pamene akakamira kukhala m'moyo wa uchimo. Nthawi zina titha kuwachosa paudindo. Vesi 21 ikutichenjedza kuti titsachite izi ndi kungofuna kupudza koma tichite izi ndi umboni weniweni.

C. tidzapewa mavuto ambiri mumpingo tikatsatira zomwe zikuphunzitsidwa pa vesi 22. Tikhale ochenjera potsankha atsogoreri athu. Muwayetse iwo ndipo titenge nthawi yathu kuwapempherera ndi kutsara chakudya kenako titsankhe atsogoleriwa. Machitidwe 14:23, 1Tim.5:24 ikuti ndi anthu ena sikovuta kuzindikira machimo awo koma anthu ena ndiovuta kudzindikira machimo awo. Tikhale otsamala ndipo tipereke chidzudzulo pamene chilikufunikira.

11. Paulo pa chaputala 6:3-10 akumuudza Timoteo kukhala patali ndi ophunzitsa ziphunzitso zonyenga komanso amene amayambitsa phokotso mumpingo. 1Yoh. 1:10-11

A. Paulo akuphunzitsa kuti cholinga cha aphunzitsi onyenga ndikupedza ndalama. Onani vesi 7 kuti muone chiganidzo choyenera kuti anthu ambiri safuna kukhala okhulupirira. Vesi 8 ikutiphunzitsa kukhala okhutitsidwa ndizomwe tilinazo m'moyo wathu. Vesi 9 ikunena kuti iwo amene amakhumba chuma amagwa munsampha ndipo monga vesi 10 ikunenera chimawapititsa kuchionongeko. Chifukwa chake ndichakuti anthu ambiri kufunafuna chuma ndi chinthu choyamba m'moyo mwao ndipo amanva kuti alibe ndalama zokwanira.

B. Paulo akunena za akulu ampingo. Zikukhala ngati amanena ndi abusa akuno ku Uganda. Amatsutsa iwo amene amagwiritsa ntchito mpingo pofuna kulemera.

12. Paulo akupitilidza mu vesi 11 kulangidza aphunzitsi onse ndi azilaliki onse kuti asatenge ziphunzitso za bodza komanso atsagwiritse ntchito udindo wao kuti alemere. M'malo mwake aonetsa chilungamo ndi kuyetsetsa kulimbana nako kwabwino.

13. Paulo akuphunzitsa pa vesi 17-19 kuti kulemera sikolakwika ngati chumacho wachipedza moyenera komanso ukuchigwiritsa ntchito moyenera. Osanyada chifukwa cha chuma

chomwe uli nacho, komanso otsatsiya chikhulupiriro chako pa ndalama. Kumbukila kuti chumacho chimachokera kwa Mulungu ndipo khala opatsa pogawira ena chuma chakocho. Munthu amene adayambitsa kampani ya katapila adapereka ndalama za nkhaninkhani ku mpingo pamene adayamba kampaniyi ndipo Mulungu adamudalitsa kwambiri ndipo pano ndi kampani yaikulu mu Uganda ngakhale pano kampaniyi tsiikulamulidwa ndi munthu oopa Mulungu.

## AKOLINTO WACHIWIRI (2 AKOLINTO)

Kalatayu adalembedwa kufuna kupitiridza kulimbikitsa ndi kulangidza Timoteo. Adadziwa kuti nthawi nyengo zolimba zikubwera kotero adafuna kulimbikitsa Timoteo komanso mpingo. Paulo adali kundende katangotsala kanthawi kochepa kuti anyongedwe ndipamene amalemba kalatayu, yomwenso ndi kalata yotsilidza kulemba mu moyo wake. Nero adali mfumu ya ku Roma kotero amadzunza akhristu kwambiri.

1.chinthu  choyamba kuchiyang'ana chili pa vesi 5 muchaputala choyamba. Tikuona kuti amai ndi agogo a Timoteo adali okhulupirira. Zikuonetsa kuti adagwira ntchito yophunzitsa Timoteo zokhudzana ndi Yesu. Banja lililonse la chikhristu lili ndi udindo ophunzitsa ana awo zinthu zokhudzana ndi Yesu. Muli zambiri mu Baibulo zomwe tingaphunzitse ana zokhuudzana ndi Mulungu. onani Masalmo 34:11 mwachitsanzo. Mudzayankha kwa Mulungu pachilungamo chanu pa nkhani imeneyi. Mulibe udindo ovomeredza Yesu m'malo mwa ana anu, koma muli ndi udindo wophunzitsa anawa. Anthu ambiri amene amakhala akhristu amatembenuka akadali achiche[ere msinkhu.

2. Paulo pa chaputala choyamba akupitilidza kulimbikitsa Timoteo.

A. Paulo pa vesi 7 akuti titsaope munthu.

B. Paulo akupitilidza pa vesi 8 kuwaudza okhulupirira kuima nganga panthawi ya matsautso. Pa vesi 12 akuwakumbutsa kuti atsachite manyazi ndi manzunzo omwe akudutsamochifukwa cha chikhulupiriro. 1Petro 4:12-16. Paulo akuti tikufunikira Yesu kuti atithandidze panthawi ya mayetsero.

3. Paulo mu chaputala cha 2 akupitilidza kuwalimbikitsa anthu kukhalabe muchikhulupiriro ngakhale akudzunzika. Akunena mu vesi 3-4 kuti ndi ife asilikali mu khamu la ankhondo a Mulungu. mazunzo komanso kuopsedzedwa ndi mdani ndichifukwa chakuti tili mu nkhondo ya muuzimu. Vesi 6-7 akunena kuti pali mphoto chifukwa chakupirira kwathu. Mphoto ya akhristu ndi yamuyaya.

A. mu 2 Timoteo 2:8-13 Paulo akulimbikitsa azibusa kupirira matsautsochifukwa cha anthu ake. Mu vesi 10 Paulo akunena kuti adazunzika chifukwa chofalitsa uthenga wabwino, ndipo abusa akuyenera kuchita chimodzimodzi, potsawiringula ndi cholinga chofuna kuthandidza otsankhidwa a Mulungu; kuwathandidza kuti alandire chipulumutso. Vesi 11-13 akutiudza kuti ife akhristu tidzunzika ndi Yesu ngati tikufuna kuti tikalamule naye limodzi. Mau oti "ngati timukana iye, Iyenso adzakana ife" ndi chenjedzo lokhudzana ndikuti titsagwe muchikhulupiriro, kapena muchikhristu. Vesi 13 ndi vesi ya chilimbikitso kwa ife. Ikutiudza kuti pamene ife akhristu tili okhulupirika Yesu adzakhala okhulupirika nthawi zonse. Kumbukirani kuti Yesu adazunzika chifukwa cha otsankhidwa a Mulungu. sakufunsani inu kuti muchite chilichonse chomwe iye sadachichite.

4. chaputala cha 3:1-4 akulotsera zonse ziwiri (vesi 12) matsautso kwa akhristu ndi ziphunzitso zonyenga. Ziphunzitso zikuluzikulu mu Chipangano Chatsopano ndi

tiyembekedzere matsautso ndi madzunzo komanso kuti kudzabuka ziphunzitso za bodza. Werengani vesi 1-9 ndikuona kuti Paulo walongotsola za mpingo wa ku Malawi.

A. Paulo akutiudza pa vesi 5 kuti tionetsetse ngati abusa kapena aphunzitsi athuwo ndi akhristudi. Tisakhale limodzi ndi abusa kapena aphunzitsi amene akuphunzitsa zinthu zimene sizichokera mu Baibulo. Izi zikutanthaudza kuti tiyenera kuwaedza abusa kapena aphunzitsi athu poona ngati zomwe akuphunzitsa zikufanana ndi zomwe Baibulo likunena.

5. chaputala 3:16-17 ndi mbali imodzi yotchuka kwambiri ya mu Baibulo, ndipo ndikwabwino kulowedza mavesi amenewa. Mau a Mulungu, kuyambira Genesis mpaka Chivumbulutso ndi Mau enieni a Mulungu, ndioona ndipo ali ndi ulamuliro. Cholinga chophunzira Baibulo m'mene tingathere ndicho kuti ife tikhale akhristu enieni. Timaphunzira Baibulo kuti tipembedze Mulungu ndi kumutumikira Iye moyenera. Ichi ndi chifukwa tili ndi kalasi lathuli.

6. Paulo akupitiridza pa chaputala cha 4 kulangidza Timoteo ndi abusa onse kulalikira mau a Mulungu mokhulupirika ndikukonzeka kuchita izi nthawi iliyonse. Vesi 3-4 ikukamba za mipingo lero pamene anthu amafuna kunva uthenga otsangalatsa otsati kunva za chiphunzitso cholamitsa, kuchokera mu Baibulo monga vesi 5 pamene tikuudzidwa kuti tipirire matsautso. Anthu amafuna kuputsitsidwa ndi uthenga otsangalatsa m'malo mwa ziphunzitso zenizeni za Mulungu.tilalikire pofuna kutsangalatsa Mulungu otsati munthu. maganidzo athu onse amangililidwe pa Mulungu. pakuphunzitsa zoona za Mulungu, tidzadzunzidwa ndi munthu koma tingopirira ntsautsoyi.

A. Mau a Paulo pa vesi 6-8 akhale chilimbikitso kwa tonsefe. Paulo adadzindikira kuti imfa yake yayandikira ndipo ali okhutira kuti mwakuyetsera ndi mphanvu zake watumikira Mulungu mokhulupirika ndipo ndiokonzeka kupita kumwamba. Awa ndi mau a chigonjetso a Paulo munthu amene wadzunzika kwambili ndicholinga chofuna kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu. Paulo adaphedwa atangomalidza kulemba kalatayi maka mawuwa.

B. tikuona mu vesi 9-18 chinthu china chomwe mkhristu wina aliyense ayenera kuchikonzekera.

i. tikuona mu vesi 10 ndi 16 kuti nthawi zonse pamene tikumana ndi mayetsero ndipo mukufuna chithandidzo cha akhristu ena, iwo amakuthawa. Mat. 26:31.

ii. anthu ena kutengera vesi 14 azakuputani ndi kukuvulazani.

iii.Mulungu adzakhalabe ndi inu sadzakuthawani. Iye kutengera vesi 17 ndi 18 adzakulimbikitsani panthawi yanu ya mayetsero. Nthawi zonse yang'anani pa Mulungu.

## TITO

Paulo adalemba bukuli zaka zoyambilira kutsiyana ndi buku la 2 Timoteo. Akulembera kwa Tito yemwe adali mtsogoleri wa mpingo wachichepere. Adakhudzika ndi ziphuzitso zachinyengo zomwe zinali zikupitirira ndi kutsowa kwa ntchito za bwino mwa akhristu.

1.Paulo pa chaputala 1:5-9 akulangidza Tito kutsankha akulu ampingo ndipo akumupatsa malangidzo azowayeneredza anthu omwe angawatsankhewo. Chiphunzitso chomwechi tikuchiona mu kalata yake yopita kwa Timoteo. Ndikofunikira mpingo kukhala ndi atsogoleri oopa Mulungu. akunena pa vesi 7 zomwe wayankhula mu buku la Timoteo kuti mkulu wa mpingo akhale ndi Mbiri yabwino. Akhale ndi moyo wa chitsanzo. Vesi 9 ikuti mkulu wa

mpingo aphunzitse Mau a Mulungu mokhulupirika kuchokera mu Baibulo, ndikutetedza chiphunzitso kuti anthu ena asachipotodze.

A. vesi 10-15 akunena za adani amene ali mumpingo ndi atsogoleri ake. Chifukwa chomwe tikufunikira atsogoleri abwino ndichakuti monga Paulo akunenera kutetedza mpingo kwa aphunzitsi onyenga. Adalongotsolapo zina za chiphunzitso chonyenga. Paulo pa vesi 7 ndi 11 akutsutsa za anthu omwe amaphunzitsa ndicholinga chofuna ndalama. Ngati atsogoleri cholinga chathu ndikutumikira Mulungu kuti ufumu wake upite patsogolo koma otsati tikhale ndichuma.

B. vesi 16 ikuphunzitsa kuti atsogoleri ambiri amakamba nkhani zokoma zokhudzana ndi akhristu abwino pamene miyoyo yawo siinaonetsa kuti ndi akhristu enieni.

2. chaputala 2-3 tikuonapo malangidza amomwe tingakhalire ngati akhristu m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Tichite ntchito zabwino chifukwa ndife opulumutsidwa; otsati kuti tipulumuke.

A. vesi 1-8 tikhale zitsanzo zabwino kwa ena, ndipo akulu ali ndiudindo waukulu wakuchita izi. Vesi 14 ikuti tikhale ndi chidwi chochita ntchito zabwino.

B. chaputala 3:1 tikuudzidwa kukhala nzika zabwinondi kunvera Malamulo adziko lathu.

C. chaputala 3:10 ndi malangidzo amomwe tingachitire ndi munthu odzetsa mgawaniko. Timuchenjedze iye ndipo ngati sakunvera iye ayetsedwe wakunja. Tiyenera titsamalire ndikutetedza mpingo.

## FILEMONI

Iyi ndi kalata yaing'ono yomwe Paulo adalemba m'malo mwa mkhristu wa tsopano. Mkhristu wina dzina lake Onesmasi adali kapolo ndipo adaba ndalama kwa mbuye wake nathawira ku Aroma. Adakumana ndi Paulo nasandulika kukhala mkhristu ndi nzache wa Paulo. Paulo adamuudza Onesmus kuchita chinthu cholongotsoka ndiko kubwerera kwa ambuye ake. Paulo adalemba kalata kwa mbuye wake Filemoni kumupempha kuti achitire chifundo Onesimasi amene ndi mkhristu nzathu. Tsitikudziwa zotsatira za kalatayi kuti pamapeto pake zinthu zinatha bwanji.

Awa ndi mathero a mabuku okwana 13 amene Paulo adalemba mu Chipangano Chatsopano. Dziwani momwe Paulo amayambira kalata yake kuti amayamba ndi moni kenako pamapeto pake amatsilidza ndi kutsadzika momwe mukhalanso dalitso.

## AHEBRI

Palibe amene amadziwa yemwe adalemba bukuli. Lidalembedwa kupita kwa Ayuda, koma sitikudziwa ndi gulu liti la Ayuda ngakhale tikudziwa kuti limapita kwa Ayuda achikhristu kuwalimbikitsa kukhalabe muchikhulupiriro otsabwerera kuchipembedzo cha chiyuda. Muli maphunziro ofunukira kwambiri kwa ife mu bukuli. Limodzi mwa maphunzirowa ndi kuwonetsa kupambana kwa Yesu Khristu pa msembe za Chipangano chakale.

1.chaputala 1:1-4 ndi nfundo yaikulu kwambiri yofanana ndi ya mu Yohane 1:1-5 kutsimikidzira kuti Yesu ndi Ambuye. Vesi 2 ikubweredza zimene Yohane chaputala cha 1 akunenera kuti zinthu zonse zinalengedwa ndi Iye. Wolemba buku la Ahebri, akutsindika kwambiri pa mfundo ya kupambana kwa Khristu. Vesi 1-2 akunena za momwe Mulungu

mbuyomo adayankhulira kudzera mwa aneneri, koma pano akuyankhula kudzera kwa ife kudzera mu njira yopambana ndiye Yesu. Ayuda amadziwa kuti chidule choti “m’masiku ano otsilidza” zimatanthaudza nthawi ya Mesiya.

A. gawo lotsatira, vesi 5-14 akulongotsola kuti Yesu ndi opambana kupotsa angeloamene monga vesi 14 ikunenera ndiotumikira Yesu ndi anthu. Angelo siopambana kupotsa munthu ndipo amapembedza Mulungu monga m’mene amachitira munthu (vesi 6). Zoonadi 1 Akor. 6:3 ikutsimikidzadi kuti ife akhristu tidzakawerudza angelo.

2. chaputala 2:1-8 akunena zambiri zokhudzana ndi angelo ndi ubale wao kwa munthu ndi Yesu. Tikudziwa kuchokera mu chaputala 1:14 kuti angelo akatitumukira ife pamodzi ndi Yesu, koma 2:7 akuti kwakanthawi kochepa Yesu wadzichepetsa kupotsa angelo. Izi ndizakanthawi kochepa chabe. Dziwani 2:2-3 ndi chenjedzo la mphanvu kwa ife. Titsakane chipulumutso cha Mulungu chomwe akupereka kwa ife chifukwa sadzachiperekanso ichi kachiwiri.

A.  vesi 9-18 tikuphunzirapo za umunthu wa Yesu ndi momwe amalumukidzirana ndi ife. Tinvetsetse kuti Yesu adabadwa munthu komanso Mulungu nthawi imodzi yomweyo. Vesi 13 akunena za momwe Yesu amagawana nafe zinthu zonse monga nthenda, njala, ndi mayetsero (amene Iye sadagwemo).ndikupyorera mu imfa ya munthu wangwiroyi kuti mphanvu za Satana zaonongedwa ndipo monga vesi 15, ikunenera tidapulumutsidwa nkamwa mwa Satana. Vesi 16 ikuti Yesu adagwira ntchito yapantanda chifukwa cha munthu otsati angelo. Angelo achitayikowo sadzapulumuka kumachimo awo, koma ife titha kupulumutsidwa.

B. vesi 17-18 tikudzidwa za chifukwa chomwe Yesu adali munthu ngati ife kuti msembe yake chifukwa cha machimo athu ikalandilidwe kwa Mulungu. vesi 17 ikuphunzitsa kuti chilango cha Yesu chidalandilidwa ndi Mulungu ngati chilango cha machimo athu, mwanjira ina Yesu adadzunzika chifukwa cha machimo athu. Vesi 18 chilango cha Yesu chidalandilidwa pamaso pa Mulungu chifukwa Yesu adali otsachimwa. Ngakhale adayetsedwa monga m’mene tikuyetsedwera ife, koma iye sadachimwe. Onani Ahebri 4:15. Kumbukirani Yesu adali munthu weniweni ndipo amakumana ndi mayetsero monga zili chimodzimodzi ndi ife. Adalinso Mulungu weniweni ndichifukwa chake sadachimwe.

3. chaputala 3:1-6 tikuphunzira kuti Yesu ndiopotsa Mose. Ayuda ambiri obadwa mwa tsopano, samanvetsetsa za ubale wa pakati pa Mose ndi Yesu. Amaganidza kuti Yesu adzakhadzikitsa Malamulo a Mose kwa munthu wina aliyense. Samadzindikira kuti Yesu ndiopotsa Mose. Pamwamba pa zonse Yesu ndi Mulungu, ndipo Iye ndi amene adalenga Mose. Vesi 5-6 akutiudza kuti Mose adali wantchito okhulupirika pamene Yesu adali mwana wokhulupirika. Akulu onse a mpingo akuyenera kukhala okhulupirika podziwa kuti ndife akapolo ochepa zedi, ndipo amene tiyenera kumuika pamwamba pa zonse ndi Anbuye Yesu.

A. vesi 7-19 ndi machenjedzo kwa okhulupirira otsangodziwa ndi nzeru zathu zinthu zokhudzana ndi Yesu. Tiyenjedzere nzeru imeneyi ndikuchita zinthu zabwino pamwamba pa nzeruyi. Kungodziwa kuti Yesu ndi Ambuye sichinthu chokwanira mwaicho chokha. Timpange Iye kukhala Mulungu wathu pakumukhulupirira ndi kumudalira iye pomutsata ndi kumunvera Iye komanso kumutumikira. Vesi 19 akuti chifukwa chomwe Ahebri sakanalowa mu dziko la malonjezo ndi kutsakhulupirira. Mwanjira ina adakhulupirira Mulungu koma otsati mokwanira kuti amutsate ndi kumunvera komanso ndi motheratu kumudalira Iye.

B. Baibulo limanena za kutsiyana kwa chikhulupiriro ndi chikhulupiriro chopulumutsa ndi m’malo ambirimbiri. Chikhulupiriro chopulumutsa ndi chikhulupiriro chogwira ntchito. Tidzayankhula zambiri za izi pamene tidzidzaona buku la Yakobo.

4. chaputala 4 chikunena za kulowa mumpumulo wa Mulungu momwe okhulupirira onse adzalowemo akadzamwalira. Chenjedzo kwa ife ndilakuti kuti titsalephere kulowa mumpumulo wa Mulungu monga anthu a mu Chipangano Chakale amene adalephera chifukwa chotsanvera.

A. vesi 12 ndiyotchuka kwambiri imene imanena za mphanvu ya Mau a Mulungu, Baibulo. tidzindikire kuti ndi Mau a Mulungu ndipo kuti muli mphanvu mu uthenga wake. Phunziro ndi kuvomeredza kwa chinthu chimenechi. Chilichonse timadziwa chokhudzana bdi Mulungu chimachokera mu Baibulo. Ife akhristutiwerenge ndi kulalikira Mau a Mulungu mokhulupirika.

5. chaputala 4:14 mpanka chapitala cha 10 pali zokhudzana ndi Yesu ngati wamsembe Wankulu.

A. chaputala 4:14 tikuona ganizo loti Yesu ndi wansembe wankulu ndipo pani ali kumwamba. Yesu ndi wamsembe wankulu ndi wangwiro chifukwa adayetsedwa monga ife koma sadachimwe. Kotero timafikira Mulungu chifukwa tayeretsedwa ndipo tayetsedwa achilungamo chifukwa cha msembe yomwe adapereka kwa ife.

B. Chaputala 5:1-10 akuyerekedza Yesu ndi anthu amene amakhala amsembe kuntundu wa alevi amene amapereka msembe za machimo a anthu ndi machimo awo. Yesu adali wa ku ntundu wa Ayuda ndipo adatsankhidwa kukhala wamsembe wamkulu ndi Mulungu. monga vesi 9 ikunenera msembe ya Yesu ndiyokwanira kubweretsa chikhululukiro cha machimo athu chifukwa Iye motsiyana ndi ansembe enawo adalibe uchimo uliwonsekotero Yesu sadafune chikhululukiro cha machimo chifukwa adali otsachimwa. Amsembe enawo adalinso ndi machimo omwe amafuna kuti akhululukiridwe.

C. vesi 11-14 mpaka chaputala cha 6 pali kutsutsa za otembenuka mtima a chiyuda. Awa ndi akhristu otsakhwima ndipo tsamakhala m'makhalidwe amene akhristu amayenera kukhalira. Pali chenjedzo apa kuti tidziwerenga Baibulo kuti tikule muchikhulupiriro. Tidzikha m'moyo woonetsa kuti ndiife a Khristu. Ndipo tikhale tikukula pang'ono ndi pang'ono kuti makhalidwe anthu adzifanana ndi zofuna zake.

D. chaputala 6:4-6 pali chenjezo kwa anthu omwe amangodziyerekedza kuti ndi akhristu, pamene si akhristu enieni. Chenjezo ndilakuti kupita kutchalitchi ndikukhala muchiyanjano ndi mpingo sidzingakupatseni chipulumutso. Ganidzo ndilakuti kungolawa (vesi 4) Yesu sikokwanira koma tiyenera (vesi 7) kumwamwa ndi kumulowetsa Iye nthupi lathu. Anthu akakhala kuti agwa zenizeni zija amatsutsidwa chifukwa amakanirira kulandira msembe ya Yesu. Anthuwa amadziwa za Yesu koma salola kukhala akhristu.

E. Chaputala 7 akufanidzira Yesu ndi Melkizedeki mkulu wina wa amsembe. Onani Genesisi 14:18-20 pamene timawerenga kuti Melkizedeki adali wamsembe wotsiyaniranako ndi amsembe achilevi. Tikudziwa kuti adali opotsa Abrahamu chifukwa anamudalitsa iye ndipo kuti Abrahamu adapereka chakhumi kwa Melkizedeki. Amene ali wankulu amapereka dalitso kwa omwe ali pansi pake. Melkizedeki adali wa msembe komanso mfumu wa ku Salemu, lomwe ndi dzina lakale la ku Yerusalemu. Dzina lake lidapangidwa ndi mayina awiri achihebri. Meleki akutanthaudza mfumu ndipo Zedek akutanthaudza chilungamo.

i. vesi 13-28 akunena kupotsa kwa unsembe wa Yesu Khristu. Izi zili chomwechi chifukwa unsembewu ndi wamuyaya.

F. chaputala cha 8 akutiudza kuti Pangano la tsopano ndilopotsa pangano lakale. Pangano lakale linakhadzikika pa chilamulo pamene pangano la tsopano lakhadzikika pa Yesu ndipo

latsindikidzidwa ndi mwazi wake. Vesi 1 ikunena kuti pangano latsopano lakhadzikika pazinthu za kumwamba pamene pangano lakale limagona pazinthu zapansi pompano. Onani vesi 6 imene imanena kuti pangano latsopano ndilopotsa komanso limatipatsa malonjezo abwino. Kotero lachotsa pangano lakale.

G. Chaputala cha 9 chikufanidza Yesu ndi chihema. Mwanjira ina chaputalachi chimafanidzira Chipangano Chatsopano ndi Chipangano Chakale kapena chipangano chakale chalamulo. Tikuona kupotsa kwa chipangano chatsopano kutsiyana ndi chakale.

i. vesi 1, 11, 24; malo achihema chenicheni ali padziko lapansi pompano. Koma chihema choona ndimalo okhalapo a Mulungu kumwamba.

ii. vesi 7ndi 12 akuphunzitsa kuti chpangano chatsopano ndi chotsatha kutsiyana ndi chipangano chakale.

Iii.vesi 12 pansi pa chipangano chatsopano machismo onse akhululukidwa kutsiyana ndi machismo ochepa chabe muchipangano chakale.

iv.vesi 13-14 akutiudza kuti msembe za nyama zimadzetsa chiyero chakunja kwa thupi. Koma nsembe yopotsayo imampanga munthu kumuyeretsa mu uzimu, muntima ndikutibweretsa pamaso pa Mulungu angwiro ndi opanda banga.

v.vesi 15-28 akunena za chipangano cha tsopano. Chipangano chakale ndi chipangano cha chilamulo. Chipangano cha tsopano ndi chipangano cha chisomo. Kutsiyana ndi chipangano cha kale chipangano chatsopano ndi chamuyaya. Nsembe ya ngwiro ya Yesu ndimsembe yokhayo yotsilidza yomwe imafunikira.

H. Chaputala 10:1-25 tikuudzidwa kuti nsembe yomwe Yesu adapereka ndiyokwanira kunthawi zonse. Pamene Yesu adali pantanda adapedza chipulumutso cha machimo omwe ana ake adachita. Machimo amkhristu adakhululukidwa kwamuyaya.

I. chaputala cha 10:26-39 akuchenjedza anthu kuti asakane chipulumutso choperekedwa kudzera mwa Yesu poganidza kuti pali chipulumutso china chomwe tiyenera kuchidikira otsati chilipochi. Chikhululukiro kupyorera ku msembe ya Yesu khristu ndichipulumutso chomwe tilinacho. Vesi 26 ndi chenjezo lolandira chipulumutso chomwe chaperekedwa ndi nsembe ya Yesu pompano chifukwa ngati sititero sipadzakhalanso mwayi wina womwe udzapedzeke. Anthu amafuna kuchita zinthu munjira yao kuphatikidza kudzipangira chipulumutso paokha. Umodzi mwa umboni oti nkhani ya Yesu m'Baibulo ndiyoonadi ndi chakuti anthu sakadalemba kumanena za Mulungu odzichepetsa amene adamenyedwa napachikidwa pantanda.

i. vesi 27-31 akulonjedza chilango choopsa kwa onse amene akukana Yesu. Onani vesi 31 kuti muone mau omwe akutipatsa chenjezo kuti tiliganidzire ndi kuganidzira choti tichite. Vesi 28 tikuphunzira kuti kudali chilango choopsa kwa onse amene adanyodza Mose amene adali munthu wamba; ndiye tangoganidzirani ndichilango chotani tidzachilandire chifukwa chonyodza Yesu amene ali Mulungu.

6. chaputala 11 chikukamba kwambiri za chikhulupiriro. Vesi 1 ikutipatsa tanthaudzo la chikhulupiriro. Chikhulupiriro ndikudalira chinthu chomwe sitichiona kapena kuchigwira monga ngati kuika chikhulupiriro chathu chonse patsogolo lathu lonse mwa Yesu. Chaputala 11 chikuonetsa oyera onse achipangano chakale amene adali okhulupirika ndipo ndikwabwino inu kuona ndandanda wa anthuwa. Ndimeyi ikunena za anthu a chipangano cha kale, koma vesi 36-37 ikulotsera za akhristuomwe mtsogolomo adzakhale akuyenda

m’chikhulupiriro. Mavesi awiriwa amalongotsola chomwe chidachitika ndi chomwe chikuchitika ndi akhristu ambirimbiri. Tikunzekere kudzunzika ngakhale kufa kumene chifukwa cha chikhulupiriro chathu mwa Yesu.

7. chaputala cha 12 chikutiudza kutsaleka kuyang’ana pa Yesu.

A. Vesi 1-2 ikulongotsola kuti tili ndi zitsanzo za akhristu omwe adamwalira titsadakhale ife kuphatikidza anthu onse omwe ali pa ndandanda mu chaputala cha 11kutithandidzira ife kukhala monga m’mene iwo amakhalira. Tikulangidzidwanso kuyang’ana nthawi zonse pa Yesu kuti atithandidze m’moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Tidziutenga moyo ngati masewera ofunikira kupirira. Anthu ambiri amakhala kanthawi kochepa kutsanzira akhristu koma pamapeto pake ndi kugwa. Mkhristu weniweni ndi iye amene amayang’ana pa Yesu kuti amuthandidze iye kukhala monga mkhristu m’moyo wake onse potsawerengera ntsautso yomwe akukumana nayo. Vesi 3 ikubweredza ganidzo loti udindo wathu ndi kufatsa ndi kupirira mpaka pamalekedzero pa moyo uno.

B. vesi 4 ikutiudza kukhala okonzeka ngakhale kukhetsa mwazi wathu ngati kungafunikire kutero polimbana ndi tchimo. Chikhulupiriro chidzakuthandidzani kupirira.

C. vesi 5-13 ikutiudza kuti nthawi zina timadzunzika chifukwa Mulungu akutilanga. Chilango cha Mulungu ndi umboni oti ife ndi anthu ake. Werengani Miyambo 3:11-12. Ngati sanakulangeni chifukwa cha tchimo lochita mobweredzabweredza kapena tchimo lotsalapidwa ndiye kuti inu simuli ana ake.

D. vesi 14-17 ikutikumbutsa kuti tikhale ndi makhalidwe omwe adzionetsa kuti ndi ife ana a Mulungu otsati anthu adziko lapansi. Tikhale ndi Mbiri yabwino pamene tikhala m’moyo wotsanzira hitsanzo cha Yesu. Sitimapulumutsidwa ndi khalidwe labwino koma khalidwe labwino limakhala umboni oti ndi ife ana a Mulungu ndipo tinapulumutsiwa ndi iye.

E. vesi 18-24 ndi kufanidzira pakati pa chipangano chakale ndi chatsopano.

i. chipangano chakale sichimapereka chitonthodzo chifukwa nthawi zonse chimatikakamidza kuyandikira Mulungu. Mose pa vesi 21 analilongotsola panganoli ngati chinthu chochititsa mantha. Anthu amaopsezedwa ndi imfa pamene Mulungu wayankhula ndi iwo (Eks. 20:19). Adaopsedzedwa ndi imfa ngati akanangogwira Phiri limene Mulungu adali (Eks. 19:13).

ii. chipangano chatsopano chikulongotsoledwa ngati chotipititsa ife pafupi ndi Mulungu (vesi 22-24); Tili ndi mwayi ofikira Mulungu kudzera mwa Khistu Yesu. Tikuona kulongotsola kwa nsonkhano wa anthu achilungamo kumwamba. Chipangano chatsopano ndi chodzetsa chimwemwe kutsiyana ndi chakale. Nkulu wa ansembe adali pakati pa anthu ndi Mulungu pansi pa chipangano chakale. Muchipangano chatsopano, timapita popedzeka Mulungu mwa ife tokha.

F.Kumathero kwa chaputachi chikutsilidza ndi mavesi 25-26 pamene akutiudza kuti tisakane zochenjedza zochokera kumwamba chifukwa monga chaputalachi chikutsilidzira Mulungu wathu ndi Mulungu wachilango choopsa zedi.

8. chaputala 13 vesi 1-6 akutseka bukuli ndi kamulu ka Malamulo amene tiyenera kuwanvera.

A. vesi 1 akutiudza kuchita chikondi chapa abale.

B. vesi 2 akutiudza kulandira bwino alendo.

C. vesi 3 akutiphunzitsa kuti akhristu onse ndi thupi limodzi ndipo pamene mkhristu modzi avutika ndiye kuti tonse tavutika. Mwachitsanzo pamene mkhristu nzathu waponyedwa mundende chifukwa cha chikhristu kuli ngati tonsefe taponyedwa mundende chifukwa cha m'modziyo. Tichite monga tingathere kuti tithandidzepo. Kwambiri chachikulu chomwe tingachite ndikupempherera munthu otereyo.

D. vesi 4 ikutipatsa Malamulo opanga banja lathu kuti likhale la ulemu pankhani zogonana.

E. vesi 5 akutiudza kuti titsakonde ndalama. Tikhale okhutitsidwa ndizomwe Mulungu watipatsa.

F. vesi 6 timaona moyo ndi chilimbikitso chifukwa Yesu ali mbali yathu. Timachita chilichonse ndi mphanvu chifukwa Yesu ali ndi ife. Ngakhale imfa siingativuladze.

9. vesi 7-17 pali malangizo ambiri kwa ife. Titsatire atsogoleri athu ndi kupewa aphunzitsi achinyengo. Vesi 8 ikunena kuti tiyang'ane pa Yesu chifukwa iye samasintha. Vesi 16 ikutiudza kuti tidzichita zinthu zabwino; chifukwa zinthu zimenezi zimakondweretsa Mulungu.

10. vesi 18-25 olembayu akumalidza bukuli ndi pempho kuti akhristu adzipempherera atsogoleri awo amene akunenedwa pa vesi 17 kuti akhale overa. Kotero tikhulupirike popempherera atsogoleri athu.

A. Vesi 20-31 ndi madalitso. Madalitso ndi mafuno abwino kuchokera kwa Mulungu operekedwa kwa anthu ndi wansembe muchipangano chakale. Kapena mbusa wa chikhristu. Lev. 9:22-23. Pali madalitso ambiri amene amapedzeka mu Baibulo.

Cholinga cha buku la Ahebri

1. Kuonetsa kupambana kwa Yesu kupotsa zolengedwa zonse monga angelo ndi Mose.
2. Kuonetsa kuti Yesu ndi mkulu wa msembe wathu ndipo ndiopotsa amsembe ena onse.
3. Kupotsa kwa pangano la tsopano kutsiyana ndi lakale lija.

## YAKOBO

Yakobo ndi buku lomwe limapereka malangizo a zinthu zenizeni zochitika. Bukuli limakamba za okhulupirira a chiyuda amene pothawa chitsautso cha akhristu adamwadzika m'madera ambirimbiri padziko lapansi. Cholinga cha bukuli ndi kulimbikitsa owerenga kukhala m'moyo wofananandi chikhristu otsati mumangotchuka kuti ndi ife akhristu koma muntima tisakuchita chomwecho. Muli malangidzo ambiri anzeru achikhristu mubuku limeneli komanso ulangidzi okhudzana ndi tchito zabwno. Ndi buku lomwe likunena za zinthu zochitika.

1.chaputala 1:1-8 mayetsero, chipiriro, nzeru, ndi chikhulupiriro.

A. vesi 2-3 zimapitira limodzi. Vesi 2 payokha ndi lamulo lachilendo kwambiri. Phunziro ndilakuti Mulungu amatumidza mayetsero pofuna kuika mwa ife kufatsa ndi komanso kuti tikhale okhwima munzeru. Ntsautso ndi yabwino kwa ife chifukwa imabereka chimwemwe. Tikudziwa kuti kuchokera mu buku la Aroma 8:28ntsautso imatibweretsera ubwino.

B. vesi 5-6 akutiudza ife kufunsa neru kwa Mulungu, ndikumudalira iye pamene tamufunsa chomwechi. Pempherani ndi kufunsa Ambuye kuti akutsogolereni, ndipo ndi chilimbikitso muchite zonse ndi nzeru zomwe wakupatsani.

2. chaputala cha 1:9-18 chuma, mayetsero, kubadwa mwatsopano.

A. vesi 9-11 akutiudza kuti titsamazinve ndi momwe talemerera, chifukwa chuma chathu padziko lapansi ndi chakanthawi kochepa. Ngakhala mbale otsauka atha kukondwera muumphawi wake chifukwa malo ake ali kumwamba.

B. kuthanthaudzira kwabwino kwa vesi 12 ndikwakuti munthu amene amalimbana ndi mayetsero ndi odala.

C. vesi 13-15 akukamba za mayetsero. Mulungu tsayetsa munthu. Satana amagwiritsa zikhumbokhumbo za uchimo zomwe zili mwa ife kutinyengerera nazo kuti tigwe muuchimo. 1 Akor. 7:15 tikuphunzirapo kuti Satana ndiyemwe amatiyetsa ife. Mulungu amatiyetsa ife kuti atsimikidzire chikhulupiriro chomwe chili mwa ife, ndi kuona chidwi chathu monga tikuonera mu Genesis 22 imene ndi nkhani ya mbanja yokhudzana ndi Abrahamu amene adalamulidwa kukapereka msembe mwana wake m'modzi yekha Isaki, onaninso Eks.20:20.

i. kulongotsolera bwino kwa chiyetsondikukhala ndi mwayi ochimwa ndi ganidzo loti lauchimo pamene uli wekhawekha.

ii. kulongotsolera bwino kwa mayetsero ndikukhala ndi mwayi ochimwa ndiponso kulimbikitsidwa ndi Satana kapena munthu kupitilidza kuchimwako. Mulungu sayetsa munthu.

iii.aliyense amapanga chiganidzo yekha khaya ndikuchimwa kapena kutsachimwa.sitingamude wina kuti ndiyemwe wathandidzira kuti tichimwe chifukwa chinali chisankho chathu.

D.vesi 17 ikutiudza kuti timalandila zinthu zonse zabwino kuchokera kwa Mulungu. palibe chabwino chomwe chimabwera ndi Satana.

3. Chaputala cha 1:19-27 pali natindi wa malangidzo.

A. vesi 19-21 akutiphunzitsa kukhala ndi moyo wodziletsa, zinthu zomwe tadziphunzira kale mu buku la Agalatiya 5:23 ngati chimodzi cha zipatso za Mzimu.

B. tikuona pa vesi 21-25 tiyenera kuonetsa chikhulupiriro chopulumutsa chomwe cili mwa ife ndi ntchito zomwe tikuchita. Chikhulupiriro chopulumutsa chimakhala ndi zipatso. Tiyenera kuchita chomwe Baibulo limatiphunzitsa koma otsangoyankhula kulephera kuchita. Onetsa chikhulupiriro chanu ndi ntchito, monga kuthandidza ena, kutumikira mpingo,kuthandidza ndi ndalama kumpingo ndi malo ena.

C. vesi 26-27 akunena za chipembedzo choyenera. Koyamba tikuwerenga kuti ngati sitiletsa lilime lathu, chipembedzo chanu chili chabe. Lilime lotsatetedzedwa ndi loopsa kwambiri ndipo Yakobo walikambanso kachiwiri mu chaputala cha 3ndi 5. Kenako tikuwerenga kuti chipembedzo chenicheni ndichomwe chimatulutsa ntchito zabwino otsangoti zoyankhula zopanda zipatso.

i. dziwani vesi 27 ikuti akhristu akulangidzidwa kupereka zotsowa kwa azimayi ndi anaamasiye.

4. Chaputala 2:1-13 akunena za tchimo la msankho mumpingo. Ndizotchuka mumpingo kuti anthu amaonedwa motsiyana poyang'anira chuma chawo kapena m'mene amakhalira m'mudzi mwawo. Tikumbukire kuti m'maso mwa Mulungu akhristu tonse ndi ofanana. Mkhristu wachuma kapena otsauka onse kwa Mulungu ndi chimodzimodzi.

5. Chaputala 2:14-26 akunena za maganizo akuti chikhulupiriro chopulumutsa ndi chikhulupiriro chomwe chimapita ndi ntchito. Ganidzo ndi lakuti munthu yemwe wapulumutsidwa amatulutsa zipatso za ntchito zabwino. Chikhulupiriro chopulumutsa chimadzadza ndi ntchito otsati chopanda ntchito ngati chili chopanda ntchito ndiye kuti chikhulupirirocho ndi chakufa.

A. tikuona zitsanzo za chikhulupiriro chopulumutsa kuti chimadzadza ndi ntchito.

i. vesi 15-16 tisamangowaudza anthu kuti pepani kenako kuwapempherera tikuyeneranso kuwathandidza. Mwachitsanzo ngati banja lao likudzunzika ndi njala tiwathandidze iwo ndi chakudya.

ii. katutu konse (vesi 17,20,26)Yakobo wakhala akunena kuti chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa.

iii.Yakobo pa vesi 19 akuonetsa kuti ngakhalenso ziwanda zimakhulupirira, koma sidzidzapita kumwamba.

B. ndikwabwino kukumbukira kuti tidapulumutsidwa ndi chikhulupiriro basi otsati ndi ntchito zathu. (Aefeso 2:8-9).

C. tikumbukirenso kuti Mat. 7:21-23 akutichenjedza kudziyetsa tokha ngati tili ndi chikhulupiriro chopulumutsa.

D. chiphunzitsochi ndi chofunukira chifukwa zikutanthaudza kuti m'mipingo mwathu mwadzala ndi anthu omwe sakupita kumwamba. Anthu ambiri sakuchita china chili chonse kupatula kupita kutchalitchi tsiku la Mulungu. Baibulo likulongotsola bwino kuti chikhulupiriro chopulumutsa chimakhala ndi zichitochito.Kunakakhala kuti aliyense amene akumati mkhristu anali mkhristudi kuchokera pansi pa mtima, ndikutsimikidza kuti dziko lapansi akanakhala malo abwino kukhalapo.

6. Yakobo 3:1-12 akutchula lilime. Pali phunziro lalikuli pazimene lilime lingaononge.

A. choyamba vesi 1 ikutipatsa chenjedzo lokhwima kwambiri lokhudzana ndi udindo wathu pakuphunzitsa. Ife aphunzitsi tinvetsetse kufunikira kwa mphunzitsi. Zophunzitsa zathu zitha kupititsa munthu chifupi ndi Mulungu kapena zitha kupangitsa munthu kutalikirana ndi Mulungu, ndi kulondola njira ya kugahena. Mphunzitsi akonzekere kuphunzitsa ndipo tipemphere ndi kufunsa Mulungu kuti atitsogolere pa mau ena aliwonse womwe tingayankhule pophunzitsa. Liwu limodzi lolakwika litha kuononga zinthu zambiri zomwe zingavutenso kubwedzeretsa/kukonzanso.

B. timawerenga zambiri zoyipa zokhudzana ndi lilime. Timawerenga kuti ndi chida choopsa ndi champhanvu pononga zinthu. Mau kuchokera pa lilime lathu laling'onoli atha kuononga kotheratu anthu ena. Mau amapangitsa mpingo kugawanika kapena kupangitsa anthu mumpingo kuyamba kumenyana. Vesi9-10 ikunena momwe lilime lingagwiritsidwe ntchito moyenera kapena molakwika. Lilime lathu tiligwiritse ntchito pazinthu za bwino monga kulemekedzera Mulungu ndi kumangirira akhristu anzathu.

7 chaputala 3:13-18 ndi zokhudzana ndi nzeru.

A.Mu vesi 14 Yakobo akunena zinthu zoyipa zomwe ena amachita momga msanje, kudzikonda kudzikudza ndi kunama. Vesi 15 ikunena kuti zinthu izi zimaonetsa nzeru ya Njerekedzi.

B. vesi 17-18 ikunena za ntchito za bwino zomwe zimabwera chifukwa cha nzeru zabwino zomwe zimachokera kumwamba kwa Mulungu. tipedze nzeru zathu kuchokera kwa Mulungu, ndipo izi zingatheke pamene tifunsa ndi kupempha Ambuye kuti atiyendetse munjira ya nzeru yeniyeni.

8. chaputala cha 4 ndi chabwino chofukwa cha zinthu zina zomwe zimapedzekamo.

A. choyamba chomwe chimapedzekamo chili pa vesi 1-2. Kutsirira kapene kufuna katundu wa eni ake kumabweretsa mavuto. Zimayambitsa nkhondo zambiri. Lamulo lakhumi likutiudza ife kukhala okhutitsidwa ndi zomwe Mulungu watipatsa otsati kutsirira zomwe anzako alinazo.

B. vesi 3 ikutiudza kuti mapemphero athu samayankhidwa chifukwa amakhala ndi zilakolako za kuthupi. Mapemphero athu akhale okhudzana ndi Ufumu wa Mulungu. otsati ongonena zokhudzana ndi zokhumba zathu.

C. vesi 4-10 akubweredza zomwe Yesu adanena pa Mat. 6:24 kuti sitingakhale ndi ambuye awiri nthawi imodzi. Mulungu akhale woyambirira m'moyo mwathu; chikondi chathu choyamba. Titsankhe Mulungu koyambirira kenako zinthu zina zofunikira m'moyo mwathu. Titsangofuna zinthu zotsangalatsa zilakolako zathu za kuthupi.

D. vesi 11-12 akunenanso zokhudzana ndi lilime kachitatu.

E. vesi 13-17 zokonza zathu zonse zikhadzikike pa chifuniro cha Mulungu. Zikonzero zathu zonse zidalire chifuniro cha Mulungu. Ndiumbuli, lomwenso ndi tchimo kuganidza kuti ndife olamula otsati Mulungu.

9. chaputala 5 pali zinthu zingapo zomwe tikudzionapo

A. vesi 1-6 ikutsutsa maganidzo okhala ndi cholinga choti tipedze chuma. Tikhale chifukwa cha Mulungu ndi kukhutitsidwa ndi ndalama zomwe amatipatsa. Vesi 4 akunena za tchimo lolemera ponamidza anthu ena komanso m'mene Mulungu akulitsutsira tchimoli.

i. vesi 5 tikuwerenga zamomwe anthu amakhalira m'moyo wa manyado ndi chuma chopedza munjira yonamidza anthu. Mulungu malo amiri m'Baibulo akutsutsa anthu omwe amapedza chuma munjira yonamidza anzawo. Ndikukumbutsidwa nkhani ya Lazaro ndi munthu wachuma yomwe ikupadzeka pa Luka 16:19-31. Sikolakwika kukhala olemera ngati tikupedza chumacho munjira yoyenerera, komanso chumacho sichikutilamulira, koma kuti tikugwiritsa chumacho kutumikira Mulungu.

B. vesi 12 ikukambanso za lilime. Gwiritsani lilime lanu ndi zolinga zabwino otsati zoipa ayi. Chitsanzo ndi kugwiritsa ntchito lilime lathu kukamba zinthu zoona. Ife akhristu tidzidziwika ndi kukamba choonadi.

C. chaputala 5:13-18 ndi nkhani yokhudzana ndi pemphero.

i. tikuona mu vesi 13 kuti tipemphere pamene tili muntsautso. Komanso kuti titsamangotsangalala pamene zinthu zikuyenda; komanso tiyamike Mulungu mokwedza.

ii. pamene wina adwala, tikuona pa vesi 14-15 kuti aitane akulu ampingo kuti amupempherere.ndi Mulungu amene adzamuchilitse chifukwa cha pemphero la chikhulupiriro la omwe apempherawo. Dzindikirani kuti ndi Mulungu yemwe amachilitsa otsati opempherayo. Dzindikiraninso kuti ndalama sidziperekedwa kwa akulu opempherawo.

iii.vesi 16 akunena za kukhulupirika kwa wina ndi nzache. Ndikwabwino kwa ife kukhala ndi nzathu yemwe tingamuudze za machimo athu ndi mavuto omwe tikudutsamo kuti tizipemphera naye limodzi.

iv.vesi 17-18 ndichitsanzo cha mphanvu ya pemphero la munthu olungama. Pempero la mkhristu ndi chida champhanvu kwambiri.

D.vesi 19-20 akutanthaudza kufunikira kwa kuthandidza anthu ena powabwedzeretsa ku chiyanjano ndi mpingo, kapena kuthandidza kuthandidza munthu okhulupirira kumene kumupititsa chifupi ndi Yesu. Tikuona kuti pali madalitso pochita izi.

## PETRO WOYAMBA

Petro woyamba adalembedwa kupita kumipingo yomwadzika mu Asiya yense. Bukuli lidalembedwa panthawi yomwe padali chitsautso chachikulu cha akhristu. Bukuli lidalembedwa ndi cholinga cholimbikitsa akhristu amene amakumana ndi ntsutsoyi. Petro akutsutsana mwachindunji ndi uthenga wongonena za chuma moyo wabwino ndi kupambana. Tikuphunzira kuti mkhristu adziyembekedzera kuzunzika ndinso kuti ntsutso yathuyi ili ndi cholinga pamene ili kuchitika.mulu phunziro m'bukuli lokhudzana ndi kukwanira kwa chitsomo cha Mulungu.

1.Chaputala cha 1chikuyamba ndi Petro akupereka zomuyeneredza zake. Ndi mtumwi, komanso ndi Petro yemweyo amene anali limodzi ndi Yesu.

A. Chaputala 1:4-5 ndi chilimbikitso. Tikuudzidwa kuti onse amene adaikidwa kukhala ana a Mulungu adzakhalabe ana a Mulungu, ndipo Mulungu adzachitsogolera chinthu chimenechi ndi mphanvu yake.

B. Popedza Petro watilimbikitsa ife, chaputala 1 chilinso ndi zophunzitsa zina zolimba kuyambira mavesi 6-9. Uwu ndi uthenga okhudzana ndi kuzunzika, uthenga womwe Petro waukamba mochuluka m'buku laling'onong'onoli. Muli zambili zokhudzana ndi matsautso mu chipangano chonse Chatsopano chifukwa Mulungu akufuna ife kukhala okonzeka pamene msautso ikufikira moyo wathu. Phunziro kuchokera mu Baibulo pa ganidzo lakuti ngati uli mkhristu ndiye kuti udzalemera udzakhala ndi moyo wabwino ndi wachipambano akuti zimenezi ndi zonama.

i. pali chifukwa chomwe Mulungu amalolera kuti tidzizunzika. Vesi 7 ikuti mavuto amayetsa kulimba kwa chikhulupiriro chathu. Tikumbukire kuti Mulungu amakhala Mulungu wathu pamene zinthu zikuyenda. Ngakhalenso zinthu ndizitsayenda Mulungu amakhala Mulungu wathunso. (Yobu 2:10)

C. vesi 10-12ndi gawo lokhudzana ndi maulosi kuti (vesi 10) samanena monveka bwino zokhudzana ndi chipulumutso, koma vesi 13 ikuti zidaululidwa kwa ife kupyorera kubwera kwa Yesu. Aneneri adali ndi ganidzo la chipulumutso koma samadziwa dzina la Yesu limene tikulidziwali.

D. vesi 13-21 akunena momwe makhalidwe athu angatsangalatsire Mulungu. tikukumbutsidwa muvesi 18-19 kuti tinagudwa ndi mwazi wa Yesu.

E. Tikukumbutsidwa muchaputala 1: 22-2:10 za maudindo okwana anayi omwe akhristu tili nawo.

i. vesi 22 ikuti tikondane wina ndi nzache kuti zibweretse ubwino kwa anthu ena.

ii. kachiwiri, chaputala 2:2ikuti tiyenera kukula muuzimu. Izi zimachitika pamene tiwerenga ndi kulingalira Baibulo lathu mwachidwi.

C. chachitatu vesi 5 ikuti ife akhristu ndi amsembe oyera okwanitsa kupereka msembe ya kuuzimu. Ife akhristu sitikuunikiranso wamsembe kuti atinenere zokhumba zathu kwa Mulungu. mkhristu aliyense atha kufika pamaso pa Mulungu, ndi mapemphero ndi chiyamiko, ndipo ichi ndi cholandilidwa pamaso pa Mulungu.

D. chachinayi chaputala 2:9-10 akuti lalikirani choona chokhudzana ndi Yesu. Titha kukwanitsa kuchita ichi, chifukwa cha m'mene ife tilili. Onani chimene vesi 9 ikunena zokhudzana ndi momwe ife tilili. Ndife anthu otsankhidwa ndi Mulungu ndipo talandira chifundo chake ndipo tigawe ichi kudziko lonse lapansi. Tilalikire uthenga.

3. 1 Petro 2:11-17 tikuudzidwa kuchitira onse zinthu zofanana. Tikhale ndi umboni wabwinonthawi onse. Tinvere otilamulira.

4. chaputala 3:1-7 akukambanso za ubale wa mwamuna ndi mkazi wake.

A. Akazi achikhristu akhalebe ndi amuna awo ndikuwalimbikitsa kuti alowe chikhristu. Chimodzimodzi mwamuna akakhala opulumutsidwa pamene mkazi Sali chomwechi. Onani 1 Akor. 7:13 kuti mutsimikidzire mfundo ya Baibuloyi.

B. vesi 7 ikutiphunzitsa kuti ife abambo tiwachitire akazi athu ulemu kuti ubale wathu ndi Mulungu ukhalebe. Onani Aefeso 5:25-31 kuti mutsimikidzire mfundoyi.

5. chaoutala 3:8-4:6 pali malangidzo ambiri kwa ife kuphatidza m'mene ife tingakhalire.

A. 3:8-11 tikuudzidwa kuchita zinthu zabwno kwa anthu. Ngakhale kukonda iwo amene akutichitira zooipa.

B. 3:13-14 akutifunsa ngati wina angativuladze chifukwa tachita chinthu chabwino;sitingalandire choipa chifukwa tachita chinthu chabwino, kotero titsachite mantha. Tudzadalitsidwa chifukwa cha zinthu zabwino zomwe tadzichita.

C. tikuona vesi 17 tiyenera kuchita zinthu zabwino ngakhale kuti izi zitha kubweretsa mazunzo kwa ife. Vesi 18 ikutikumbutsa kuti Khristu adazunzikanso.

D. vesi 20-21 itha motsavuta kutsainvetseysa bwino. Petro akukumbukira m'mene madzi adagwiritsidwa ntchito populumutsa Nowa ndipo kugwiritsa ntchito madzi ndi chidzindikiro kwa ife cha chipulumutso kupyorera kwa Yesu Khristu. Vesi 21 ikutchula kuukitsidwa kwa Yesu chomwe ndi chidzindikiro cha nzukiro.

6. chaputala 4:7-11 akutiudza kukhala okonzekera kubwera kwa Yesu ndi makhalidwe athu pamene tikudikira chifukwa nthawi yakubweranso kwa Yesu kachiwiri yayandikira. Werengani malangidzowa kuti muone m'mene tingakhalire pa nthawiyi.

7. chaputala 412-19 ndi maphunziro okhudzana ndi kudzunzika.

A. vesi 12 ikutiudza kukonzekera kudzunzika.

B. vesi 14 ikutiudza kuti ndife odala chifukwa tili mwa Yesu.

C. vesi 15-16 tidzindikire kuti kudzunzika kwathu sichifukwa kuti tili ndi mulandu uli onse ayi, koma kutsindikidza kuti indedi ndi ife akhristu. Timalemekedza mulungu pamene tiyenda muntsautso. Timachita izi pamene tikhala okhulupirika kwa Mulungu pokhala mu pemphero.

D. vesi 19 ikutiudza kuti tidzunzika ndithu podziwa kuti kudzunzika kwathu ndi chifuniro cha Mulungu, kotero mofatsa tipirire matsutsowa chifukwa cha ulemerero wake. Aroma 8:28 matsautso athu amatibweretsera ubwino.

8. Chaputala 5:1-4 pali malangidzo m'mene abusa ndi akulu ampingo angakhalire. Akulu ampingo tikhale ndikuthandidza komanso kutsogolera anthu athu kuti izi ziwabweretsere ubwino. Kumbukirani kuti mamembala ampingo sichida chotipanga ife kuti tilemere, ngakhale ayenera kupereka kwa mbusa wawo m'mene angathere kuti adzipedza zofunikira pamoyo wake watsiku ndi tsiku. Vesi 2 ikunena kuti timagwira ntchitoyi otsati kuti tipindule koma chifukwa timakonda Mulungu. vesi 3 ikutiudza kuti tikhale odzichepetsa otsati ophangira chilichonse. Tikhale zitsanzo zabwno kwa mamembala athu. Titsogolere anthu ndi zitsanzo zabwino otsati ndi mau owaudza iwo choti achite. Tigwire ntchito ngati akulu ampingo polondola kolona wa ulemerero amene vesi 4 akumunena. Iyi ndi mphotho yathu kutsiyana ndi chuma.

9. chaputala 5:5-11 akuyamba ndi phunziro la kulemekedza akulu, ndipo muvesi 5akunena za khalidwe la wina aliyense ngakhale wachikulire kuti akhale odzichepetsa. Zikuphunzitsidwa kumayambiriro a Baibulo kuti tiyenera kulemekedza akulu (Lev. 19:32)

A. Baibulo likutilimbikitsa kuti titsadere nkhawa (Mat. 6:25-34). Apa 1Petro 5:7 tikuudwa za chinthu chomwechi. Palibe chifukwa choti tidzidandaula chitsamaliro chathu chiri m'manja mwa Mulungu, ndipo timudalire iye kuti atitsamale ife.

B. Vesi 8-9 akutikumbutsa ife kuti Satana amapanga zomwe angachite kuti atigonjetse ife, koma tigwiritse chikhulupiriro chathu kuti timupewe iye chifukwa Satana ndi wamphanvu kotero sitiyenera kumumenya popanda thandidzo la Mulungu. tichite monga Aefeso 6:11 akunenera kuti tivale zida za Mulungu. Tikuonanso mu vesi 9 kudzunzika sichinthu chachilendo kwa akhristu.

C. vesi 10 ikutanthaudza kuti kuvutika kwathu ndi kwanthawi yochepa. Koma potsachedwa Mulungu adzatiitana ife ku ulemerero wamuyaya mwa Khristu kutanthaudza chimwemwe cha kumwamba.

## PETRO WACHIWIRI

Petro adalemba bukuli pofuna kuthandidza mpingo kutsutsana ndi ziphunzitso zonyenga. Adawaudza anthu kukhala okhwima muchikhulupiriro chifukwa ichi ndi chitetedzo chabwino chothanirana ndi ziphunzitso zonyenga. Zimakayikiradwa kuti Petro adaphedwa kanthawi kochepa atangolemba kalatayu.

1.2Petro 1:1-11njira yabwino yodzitetedzera tokha kwa aphunzitsi onyenga ndi kuphunzira m'mene tingathere zokhudzana ndi Mulungu. Tikuona ganidzoli mu vesi 2,4,5,6,8.

2. vesi 12-18 Petro adadziwa kuti potsachedwa aphedwandipo akuonetsa kuti adali ndi mtima wa mbusa woona. Tikuona izi mu vesi 13-15 pamene akunena kuti amafuna kuonetsetsa kuti ngakhale atamwalira mamembala ampingo akhodza kudzitetedza okha. Mkulu wampingo weniweni amakhudzika kwambiri ndi anthu ake kutsiyana ndi iye mwini.

A. vesi 16-18 Petro akutsimikidzira choona cha uthenga umenewu ponena kuti adali limodzi ndi Yesu panthawi ya kutsandulika kwake.

3. vesi 19-21 Petro akunena komwe kumachokera uneneri woona. Choyambirira vesi 20 ikutiudza kuti uneneri siuchokera mwa anthu, koma monga vesi 21 ikunenera uneneri woona umachokera kwa Mzimu Woyera pamene akutsogolera anthu kuneneraku. Mwanjira ina, uneneri woona umachokera kwa Mulungu.

4. chaputala 2:1-3 kachiwirinso Petro akuchenjedza kuti kudzabwera ziphunzitso zonyenga. Akunena kuti aphunzitsi onyengawa adzaphunzitsa zinthu zabodza, monga m'mene akunenera mu vesi 1kukana Mulungu. Vesi 1 ikutiudzanso kuti aphunzitsi onyenga adzabweretsa chionongeko pa iwo okha chifukwa akuphunzitsa zinthu zabodza. Vesi 3 ikuti chifukwa chimodzi cha kuipa kwa aphunzitsi onyengawa ndichauti amakhala kuti utumiki wao ndi nyambo yopedzera chuma. Mphunzitsi woona amalimbikitsidwa ndi chikondi chake pa Mulungu, otsati kulandira ndalama. Amayang'ana kumwamba kuti alandire mphoto yake. Kachiwiri tikuonanso kuti aphunzitsi onyengawa amabweretsera chipatsulo pa iwo okha. Mphunzitsi onyenga ndiyemwe amaphunzitsa zinthu zokhudzana ndi mulungu zomwe sidzipedzeka m'Baibulo. Mphunzitsi woona ndiyemwe mokhulupirika amaphunzitsa zokhazo zomwe wawerenga kuchokera m'mawu a Mulungu.

5. 2 Petro 2:4-9 koyamba akunena momwe Mulungu adalangira anthu ochimwa ngakhale angelo m'mbuyomo. Kenako akunenanso kuti Mulungu adapulumutsanso anthu olungama. Mu vesi 9 Petro akunena kuti Mulungu akudziwa momwe angapulumutsire anthu olungama, ndikulanga oyipa. Akhristu apa tikotonthodzedwa podzindikira kuti tipulumutsidwa ku mayetsero athu onse. Vesi 9 ikupitirira kunena kuti Mulungu adzalanga anthu oipa.

6. Petro mu vesi 10-18 akunena kuti zochita za anthu otsalungamadzi ndizonyansa kwambiri ndipo akuyenera chilango chokhwima.

A. vesi 10-13 akunena kuti anthu oipa choterewa amachimwa munjira yakuti angelo amene ndi amphanvu amaopa kuchimwa ngati kumeneku. Anthuwa ndi amwano kwambiri ndipo akuyenera chilango cha Mulungu.

B. chiyambi cha vesi 14 Petro akunena za machimo amene anthu amenewa amakonda kuwachita. Komabe mu vesi 17 tikuonabe kuti Mulungu waasungira malo amdima poti bii ku Gahena.

7. Petro akunena za aphunzitsi onyengawa mu vesi 19-22. Anthu amenewa amene amakondwa mu kuukira kwao ndiomwe ayandikira kuti akhale akhristu koma sidzidzatheka kukhala akhristu. Mipingo yathu ili ndi anthu ambiri amene amadziwa Yesu koma koma otsakhala mkhristu weniweni. Mateyu 7:21-23 akunena chomwe chidzachitike kwa anthu oterewa.

8. chaputala cha 3:1-9 Petro akuwudza aphunzitsi onyengawa amene amanena kuti Yesu sadzabweranso.

A. Vesi 8 ikutiudza kuti Mulungu ali ndi malingaliro ena okhudzana ndi nthawi kutsiyana ndi momwe ife timadziwira. Ndichovuta kwa ife kudikira Mulungu kufikira pamene adzaganidze kuti tsono ndinthawi yoti ndichitepo kanthu.

B. tikuona chifukwa chimodzi pa vesi 9 Mulungu akuchedwa pachifukwa. Ndi Mulungu wachifundo ndipo akufuna kupereka nthawi yokwanira kwa anthu ake kuti apulumutsidwe.

9. vesi 10-14 akuchenjedza kuti kuledza kwa Mulungu ndi kwanthawi yaitali, koma tionetsetse kuti tili okonzeka iye atsanabwerenso kachiwiri. Vesi 10 kachiwirinso ikunena za tsiku la Ambuye lomwe lidzakhale loopsa ndipo likudza mwadzidzidzi. Ngati sitikhala mkhristu mpompano Yesu atsanabwere kudzakhala kuchedwa kumupedza iye nthawi yomwe adzabwere.

10. chaputala 3:15-18 Petro akutsiridza kalatayu potiudza kuti tide nkhawa ndi anthu amene apotodza choonadi cha Mulungu pa zifukwa za iwo okha. Tidziwerenga nthawi zonse Mau a Mulungu ndi mtima ofuna kuphunzira. Maganidzo athu adzikhala kuphunzira chomwe Mulungu atiphunzitsa, otsati kuchita ichi pofuna kukwaniritsa zokonda zathu. Machitsanzo anthu ena apototodza Genesis 9:25-27 kutsimikidzira kuti anthu okuda ndi otembereredwa ndipo sikulakwa kuwachitira iwo nkhadza. Ili ndi gwero la tchimo la sankhu lomwe limachitika ku South Africa kwa zaka zambiri. Baibulo limanena kuti Mulungu amakonda anthu ake onse mofanana; potsayang'anira ntundu wao.

A. Petro kachiwiri akutichenjedza pa vesi 7 kukhala ochenjera kuti titsasocheretsedwe. Akutsendera pa vesi 18 potiudza ife kukula muchisomo ndi muchidziwitso cha Yesu. Chitetedzo choyenera kwa ophunzitsi onyenga ndi kudziwa Baibulo lathu. Ngati mphunzitsi ndi otsakhulupirika, pophunzitsa zomwe Baibulo limatiphunzitsa, ndikwabwino mofulumira kumuimitsa mphunzitsiyu, ngati idzi ndizovuta, ndikwabwno tingochoka kutsiyana ndikunvetsera ziphunzitso zonyengazi.

## MAKALATA A YOHANE-YUDA

Mtumwi Yohane adalemba makalatawa mochedwa m'moyo mwake choyamba Yohane adalemba makalatawa pofuna kutsutsa chiphunzitso chonyenga. Panali gulu lina lomwe limatchedwa Aginostikisi. Anthuwa amadzitama kuti ali ndi nzeru ya padera yomwe amayenjedzera kuziphunzitso za Baibulo. amakhulupirira kuti thupi la munthu lili ndi magawo awiri. Amakhulupirira kuti tchimo limakhala kumbali ya thupi lokha, koma Mzimu wa munthu ndiodzadzidwa ndi zinthu za Mulungu. amakhulupirira kuti sikolakwika thupi lamunthu kuchimwa m'mene lingathere, ndipo idzi sidzingakhudze Mzimu wake wa munthu. Iwo amakhulupirira kuti umadzuka ku uzimu pamene ukuphunzira zinthu zodzetsa nzeru. Anthu amenewa amakhulupiriranso kuti Yesu sadakhale ngati munthu weniweni.

1.1Yohane 1:1-4 akuyamba ngati uthenga wabwino wa buku la Yohane. Tikuwerenga pa vesi 1 kuti Yesu ndi wamuyaya. Vesi 2 akutiudza kuti Yesu adadziwonetsera yekha zomwe zikutanthaudza kuti adali ndi maonekedwe ngati munthu, ndipo kuti Mulungu adabwera kudzakhala ndi munthu. Yesu adali ndi thupi lenileni. Chiphunzisochi cholinga chake kunali kutsutsana kwanthunthu ndi awa a chiGinositikisi. Ngati Yesu sadali munthu weniweni Mulungunso sakadalandira msembe yomwe adapereka chifukwa cha machimo athu. Mulungu amafuna munthu amene sadachimwepo m'moyo wake onse kuti alangidwe m'malo mwathu kuti machismo athu akhululukidwe.

2. chaputala 1:5-10 akunena kuwunika kwa Mulungu ndi tchimo la dziko lapansi.

A. vesi 5 ikuti Yesu ndi kuwala kwa dziko lapansi ndipo mwaiye mulibe m'dima kapena tchimo. Yohane akunenanso chimodzimodzi mubuku la uthenga wabwino pa Yohane 1:4-5.

B. Yohane pa vesi 6 akuti sitingayende muuchimo ndikukhala pachiyanjano ndi Khristu Yesu. Izi zikutanthaudza kuti sitingasankhe kuchimwa mwadala ngati tili mwa Yesudi. Timayetsetsa kukhala otsachimwa nthawi zonse. Pamene timakhala kuti tikuchimwa izi zimangochitika mwangodzi koma otsati mwa chifuniro chathu.

C. vesi 8 ndi 10 tikuudzidwa kuti pamene tili ndi moyo tidzakhalabe tikuchita uchimo ndipo vesi 7 akuti mwazi wa Yesu udzakhalanso ukutsuka machimowa. Munthu aliyense amene amati alibe uchimo ndiwabodza Baibulo likunena motero.

D. mkhristu weniweni amada nkhawa ndi tchimo lake ndipo moona mtima amalapa tchimo limeneli. Vesi 9 ikutitsimikidzira kuti tidzakhululukidwa ndi Mulungu wathu okhulupirika amene adzatiyeretse pachotsalungama chilichonse mwa ife.

3. 1Yohane 2:1-17 akunena za kuyenda mu uchimo ndi mu m'dima.

A. uthenga muvesi 1 ndiwakuti okhulupirira adzayetsetsa kuti akhale m'moyo wotsachimwira Mulungu. ndipo tikakula muchikhristu sitimdzangochimwa mwachitsawawa, komanso tchimo lathu tsilikhala loopsa monga matsiku am'mbuyomu, koma kuchimwa ndiye tidzidzachimwa ndithu. Komabe Mulungu wathu wokhulupirika adzapitilidza kutikhululukira ngati tilapa moona mtima.

B. vesi 2 ikugwiritsa ntchito mau oti chiombolo cha Yesu. Izi zikutanthaudza kuti chilango cha Yesu pamtanda chinadzimitsa mkwiyo ndi kunyansidwa kwa Mulungu kotero chilango cha cha Yesu chidalandilidwa ndi Mulungu m'malo mwathu. Yesu adapereka dipo la machismo a akhristu okha basi. Aliyense yemwe sinkhristu akalandira chilango ku Gahena chifukwa cha machismo ake.

C. vesi 3-6 tikuonanso kuti timaonetsa chikondi chathu kwa Mulungu pamene timunvera Iye. Timaonesanso ichi pamene tikukhala monga momwe Iye afunira.

D. vesi 9-11 akuudza akhristu kuti akondane wina ndi nzache. Titha kutsiyana maganidzo koma mofulumira tiyanjane wina ndi nzache chifukwa timakondana.

E. vesi 12-14 Yohane akuyamikira akhrstu chifukwa chopambana pa machimo awo akale ndi ubale wao wa uzimu ndi Mulungu.

F. vesi 15-17 tikuphunzira kuti titsakonde dziko lapansi. Titsakodwe ndi zinthu zapansi pano monga ndalama, nsiriro, ndi kunyada. Ndizinthu zakanthawi kochepa. Komazinthu zabwino za Mulungu ndizotsatha.

4. mathero a chaputala cha 2 akunena za otsutsana ndi Khristundi iwo amene Sali muufumu wa Mulungu.

A. Mau oti okana Khristu akupedzeka mu vesi 18 ndipo akungopedzeka m'makalata a Yohane okha maka poyang'ana Baibulo lonse. Palibe chiphunzitso chonveka bwino chokhudzana ndi okana Khristu ngakhale pali mfundo zambiri zokhudzana ndi munthu ameneyi. Chifukwa chomwe Yohane sadatsiye poyera munthu okana Khristu ndi chakuti anthu onse munthawiyi amadziwa munthu yemwe Yohane amatanthaudza.yatitayika nzeru imeneyi kwanthawi tsopano.

B. ganidzo lomwe lili pakati pathu lero ndilakuti pali kamzimu kokana kapena kolimbana ndi chphunzitso cha chikhristu. Timadziona izi motsiyana tsiyana. Tikuona ziphunitso zambiri zotsutsana ndi Baibulo lerolino ndipo aliyense wophunzitsa motsiyana ndi Baibulo ndi Okana Khristu.

C. vesi 19-24 akunena munthu yemwe wakhala mumpingo kwanthawi yaitali ndikuphunzira zinthu zokhudzana ndi Mulungu, koma sadapulumutsidwe kotero munthuyu amagwa chifukwa sinkhristu weniweni. Mwanjira ina Mzimu Woyera sadabwere mwamunthuyu. Munthu akakhala mkhristu, vesi 20 ndi 27 tikuphunzira kuti Mzimu Woyera amabwera mwa

munthu ameneyu. Mzimuyu amatetedza munthu kudziphunzitso zonyenga ndi kugwa muchikhulupiriro.

D. chaputala 2 chikutha ndi vesi 28 kutiudza ife kuti tikhale okhulupirikabe mwa Yesu. Vesi 29 ikutiudza anthu amene ali olungama amapedza chilungamochi mw Yesu Khristu. Kuumikika kwathu pa chilungamo ndi mphatso yaulere kuchokera kwa Yesu.

5. chaputala 3:4-10 ikunena za chilungamo komanso mau amphanvu pa za tchimo.

A. vesi 6 ikuti munthu amene amakhalira kuchimwa sachokera kwa Mulungu.

B. vesi 8 amene amachita uchimo mwadala ndiochokera kwa Njelekedzi.

C. vesi 9 ikunena kuti obadwa wa kwa Mulungu sachita uchimo.

D. zotsiyana ndi izi ndi 1 Yohane 1:8ndi 10 amene amati ngati tinena kuti tilibe tchimo tidzinyenga tokha .

Kodi tingalongotsole bwanji ganizo lam'Baibuloli limene likuonetsa kuti akhristu sitimachimwa pamene malo ena likunenanso kuti anthu onse amachimwa?

Chimene Baibulo likutiphunzitsa ndichakuti pamene munthu aliyense amachimwa ndithu mkhristu moona tsamafuna kuti achimwe ndipo tsakonzekera kuti achimwe. Chitsanzo chaizi ndichakuti mkhristu atha kukhala pakutsiyana maganidzo ndi munthu wina ndikukwiya komanso kupsa mtima mpaka kuchita ndeu. Ili ndi ntchimo lomwe tikulidziwa bwino kwambiri. Komabe mkhristuyu sangadane ndi munthu ameneyu ndikuganidza zomubitsalira ndikupitiridza kumumenya. Kutsiyana kwa machimowa ndikwakuti nkhristu amachimwa koma samakonzekera kuti achimwe

Ganizo lina likuchokera mubuku la Halley's Bible Handbook tsamba 812:

Kodi tingalongotsorere bwanji ziganidzo zotsutsanazi? Pali kutsiyana pakati pamachimo ochitika chifukwa chakufoka ndi machimo ochitidwa mwadala, machimo achidzolowedzi.Khwangwala atha kudzika mapiko ake muthope, komabe adzakhala khwangwala. Munthu olungama atha kukhala ndi machimo ochitika chifukwa cha kufoka komabe adzakhala munthu olungama. Yohane zikhodza kutheka kuti adali ndi maganizo a aphunzitsa achinyengo (monga Yezebeli, Chivumbulutso 2:20) amene polalika za chiyanjano chopatulika ndi chopambana kwa Mulungu adali nthawi yomweyo kulowerera mudzoipa za kuthupi.

Pamene tili ndi moyo tidzakhala tikuchimwirachimwirabe, koma chikhumbokhumbo chathu chidzakhala kutsachita tchimo. Sitidzachita tchimo la chidzolowedzi monga chigololo lomwe nditchimo lomwe lakhala likuchitika kwanthawi yaitali. Satidzachimwa mofanana ndi momwe timachimwira titsadapulumutsidwe. Tidzadzolowera kukhala m'moyo wotsachimwa pamene oipa adzidzangotsangalala akamachita uchimo. Khumbo la mtima wathu lidzakhala kutsachitanso tchimo.

6.1Yohane 3:13-24 ndi chaputala 4:7-21 ndizokhudzana ndi chikondi.

A. vesi 13 ikunena kuti dziko silikonda akhristu m'malo mwake anthu omwe si akhristu amadana nafe. Izi zizimatithandidza kunvetsetsetsa chifukwa chomwe akhristu amadzunzidwa padziko lapansi. Timadedwa ndi anthu amene si akhristu.

B. mavesi ambiri muchigawo chimenechi akutiudza kuti chikondi ndi chinthu chofunikira kwambiri pamene munthu ali mkhristu. Chaputala 4:12 ikuti ngati tikondana wina ndi mzache, Mulungu ali nafe. Ngati mulibe chikondi ndi anzanu mwainu mulibe chikondi kwa Mulungu (chaputala 4:20).

C. chikondi chathu kwa anzathu chikhale ndithu champhanvu. Onani Yakobo2:14-18 pa chitsanzo cha chikondi cha mphanvu. Tithandidzane wina ndi nzache.

D. 1 Yohane ikutiudza m'malo ambirimbiri, kuti ngakhale tinapulumutsidwa ndi chisomo cha Mulungu, tikuyenerabe kumunvera Iye.

i. werengani machaputalaawa 2:3, 3:22, 3:24, 4:21 ndi 5:3 kuti muone kufunika komvera Mulungu.

7. 1Yohane 4:1-6 akunena zokhudzana ndi aneneri onyenga.

A. vesi 1 ikutiudza kuti kuli aphunzitsi onyenga ambiri padziko lapansi, ndipo aliyense ali ndi udindo othana ndi ziphunzitso zoterezi.

B. vesi 2 ikunena kuti tingadzindikire m'neneriwoona ndi uthenga wache. M'neneri woonayu amatenga uthenga wake wokhudzana ndi mulungu kuchokera mu Baibulo. Ife akhristu tili ndi udindo wodziwa m'neneri ngati akuyankhula zoona kapena zabodza. Timachita izi ponetsetsa kuti uthenga wake ndi ochokera kwa Mulungu. Izi ndizofana ndizomwe Mose amanena pa Deutronome 18:22 zaka 2000 zapitadzo.

C. vesi 4-5 akutiudza kuti pamene otsakhulupirira amafuna kunva ziphunzitso kuchokera kwa aneneri onyenga, ife akhristu tidzanvera ziphunzitso zokhadzo zomwe zikuchokera kwa Mulungu kudzera mukuphunzitsidwa kwa Baibulo.

8. chaputala cha 5 ndi chaputala chonena za chitsimikidza cha moyo wotsatha. Maulendo okwanira khumi Yohane wagwiritsa ntchito mau oti dziwani , Pofuna kuonetsa mfundo yakuti pali chitsimikidzo cha chipulumutso chathu. Onani 2:3, 2:5, 3:2, 3:19, 3:24, 4:13, 5:13, 5:15 ndi 5:19.

A. tikuona pa 5:4-8 phunziro lokhudzana ndi utatu wa Mulungu; Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera ndipo onse akuchitira umboni Yesu.

B. vesi 9-13 akutitsimikidzira ife kuti Mulungu anatilonjedza kuti aliyense amene akhulupirira Mwana wa Mulungu ali ndi moyo wotsatha ndipo uwu sudzachotsedwa kwa iye.

C. vesi 16 akunenanso za tchimo lotsakhululukidwa lomwenso taliphunzira mu buku la Mateyu. Ili ndi tchimo lokana kulandila Yesu ngati Mbuye ndi Mpulumutsi wathu komanso kulapa tchimo.

## YOHANE WACHIWIRI ALI NDI CHAPUTALA CHIMODZI MOMWE ZINTHU ZIWIRI ZIKUFOTOKODZEREDWA

1.vesi 1-4 akunena katsanu mau oti choona. Tikuyenera kuyenda mu choonadi.

A. vesi 1 ikuti tikondane muchoonadi zomwe zikutanthaudza kuti tikondane moona mtima.

B. vesi 1 ikutinso tingadziwe choonadi pamene tikuwerenga ndi kulingalira Baibulo lathu.

C. vesi 2 ikunena zoti choonadicho chili mwa akhristu; ife akhristu tikhale anthu achoonadi.

D. vesi 3 ikutiudza kuti chisomo cha Mulungu (kutikondera kwake), chifundo chakendi mtendere wake dzidzakhala nafe kwa muyaya. Moyo ndi wabwino kwa akhristu pachifukwa chimenechi. Akhristu ali ndi chimwemwe pamene akukhala chifukwa kulamulira kwa Mulungu kumatidalitsa ife ndi moyo wabwino.

E. vesi 4 ikutiudza kuti akhristu amayenda muchoonadi. Nthawi zonse tinene choonadi.

2. vesi 5-6 tikulamulidwa kukondana wina ndi nzache monga Yesu adatilamulira kutero pa Marko 12:31. Vesi 6 ikutiudzanso za kunvera Mulungu ndipo kuti ili ndi lamulo.

3. vesi 7-11 ndi kupitiridza za chiphunzitso cha aphunzitsi onyenga.

A. Tikuna mu vesi 7 ndi 8 kuti pali aphunzitsi ambiri omwe amaphunzitsa zotsutsana ndi chikhristu. Tidzidzitetedze tokha kwa anthu oterewa kuti atsalowerere m'mayendedwe athu ndi Yesu. Ndi mphoto kuyenda chifupi ndi Yesu kotero totsalole ziphunzitso zonyenga kuti zitsokonedze zokomazi.

B. tikuonanso kupatsula kwa ziphunzitso zonyenga. Mulungu akufuna kupanga kuti ife tidzitetedze pa ziphunzitso zonyenga kuti titsaonongeke nazo.

C. vesi 9 ikuti ubale wathu ndi Mulungu umadalira chiphunzitso cha Mulungu kukhala mbali imodzi ya ife. Ngati chiphunzitso chake sichili mwa ife kotero tilibenso Mulungu mkati mwathu. Ngati tili ndi Mau mkati mwathu ndiye kuti tilinso ndi Mulungu.

D. vesi 10 ikunena za chinthu chotsutsana ndi khalidwe lathu lolandira alendo. Tikuudzidwa kuti pamene mphunzitsi onyenga wafika pakhomo pathu titsayetse ngakhale kumupatsa moni. Tikhale ndithu achipongwe kuti tisapereke moni kapena kuuitana munthu otereyu kunyumba kwathu. Mulungu akufuna ndithu kutitetedza ife kwa aphunzitsi onyengawa. Kumbukirani kuti chinthu chomwe timakhulupirira chokhudzana ndi Mulungu ndichokhacho chomwe tikuchiwerenga kuchokera m'Baibulo.

## YOHANE WACHITATU NDI KALATA YA MALANGIZO

1.Chinthu choyamba kuchiyang'ana chikuchokera mu vesi 2-4 chomwe chikunena za pemphero. Mtumwi Yohane adapempherera moyo wabwino kwa ophunzira wake Gayo. Yohane adapempherera moyo wa thanzi ndi kukula mu uzimu. Mbusa wabwino amatsamalira moyo wa anthu ake. Sachita Nsanje pamene ophunzira wake walemera, koma amakhala okondwera ndi chuma komanso moyo wa thanzi kwa ophunzirawa.

2. Gayo adawonetsa kukula muuzimu monga akunenera pa vesi 5-8 pomwe tikunva kuti kale adagwiritsa ntchito chuma chake kutumikira Mulungu. Tikuona apa kuti ife akhristu tiyenera kuthandidza omwe akugwira ntchito ya Mulungu. chitsanzo cha izi ndikuthandidza mishonale amene akufuna thandidzo la ndalama kuti apite kudziko la chilendo kukalalikira uthenga wabwino. Thandidzo lathu kwa ogwira ntchito ya Ambuye limatipangitsa kutenga nawo gawo kuutumikiwo.

3. vesi 9-10 ikutichenjedza za mavuto otsakata omwe amapedzeka mumpingo. Muli anthu ngati Diotrefe amene amayambitsa chitsokonedzo. Anthu oterewa amakhala

otsapulumutsidwa omwe amaika chidwi chao patsogolo pa mpingo. Anthuwa amachita zinthu modzikudza. Akulu ampingo apewe mchitidwe wotere kuti atetedze mpingo wawo. Chidzudzulo choyenera chikuyenera kuchidwa pa anthu amene pofuna kutetedza mpingo ndikubwedzeretsa munthuyu ku chiyanjano cha Ambuye ndi mpingo.

4. vesi 11 ndi malangidzo kwa ife kuchita zinthu zabwino. Tikuona kuti iye wakuchita zabwino amachokera kwa Mulungu, koma munthu amene amachita choipa sachokera kwa Mulungu ndipo tsayenera kukhala mbali imodzi ya mpingo.

## YUDA NDI KALATA YAIFUPI YOMWE IKUNENANSO ZA MAVUTO A APHUNZITSI ONYENGA

1.Yuda akuyamba (vesi 1) ndikutsiridzira (vesi 24) potsimikidzira awerengi ake kuti chipulumutso chao ndi chotetedzedwa kwa muyaya; Mkhristu samagwa muchipulumutso. Akuwaudza mu vesi 1 kuti iwo "ndi otsungidwa ndi Yesu Khristu." Pa vesi 24 akuwaudza kuti Yesu adzawatsunga iwo kuti asagwe ndipo adzatiimiritsa pamaso pa Mulungu Atate wopanda chirema.

A. Vesi 20-21 ikutiudza kuti mapemphero athu ndi njira zomwe Mulungu amagwiritsa ntchito kuti atitsunge ife opulumutsidwa.

2. pa vesi 3-4 akunena kuti cholinga cha zolemba zake ndi kuchenjedza anthu zaaphunzitsi onyenga amene adali pakati. Adanena kuti iwo akulowa pang'ono pang'ono. Izinso zitipatse ife chenjedzo kwa anthu amene poyamba amaonetsa ngati athu oona a Mulungu. koma titawakhulupirira adayamba kubweretsa zonama mumpingo. Akhristu achinyengo omwe aliko lerowa poyamba amaonetsa ngati ndi achikonzedwe. Mwachitsanzo, mamomoni pachiyambi amaonetsa ndi akhristu, koma pamapeto pake mwapang'onopang'ono adaulura bodza lao lonse. Tibweredzenso kuti njira yodzitetedzera kuti titsatengedwe ndi aphunzitsi ochinyengowa ndi kuwerenga ndi kukhulupirira Baibulo lathu.

3. vesi 5-7 akulongotsola chilango choopsa chomwe chikudza kwa anthu apikitsana ndi Mulungu.

4. vesi 6-16 akulongotsola za mitundu ya kutsanvera. Iyi ndiyotsavuta kuinvetsetsa, komabe vesi 9 ndi vesi yomwe ndiyovuta kuilongotsorera.

5. vesi 17-25 ikutsilidza kalatayu pamene Yuda akutipatsa chodzitetedzera kwa aphunzitsi onyenga. Aphunzitsi onyenga atsamatidzidzimutse ife, ndipo tikonzeke kulimbana nawo.

A. Pali zinthu zinayi zomwe zingatitsunge polimbana ndi aphunzitsi onyenga.

i. choyamba chakambidwa mu vesi 20 pamene akuti tidzimange tokha pachikhulupiriro choyenerera. Izi zimachitika pamene tiwerenga Baibulo mwa chidwi kotero kuti otereyu sangatinamidze.

ii. chachiwiri chikupedzeka mu vesi 20 pamene akutimema kupemphera mu Mzimu Woyera. Mu Aefeso 6:18 talangidzidwa kale kupemphera mwa Mzimu Woyera ngati mbali yodzitetedzera kwa Satana. Ili ndi pemphero la mkhristu chifukwa tili ndi Mzimu Woyera yemwe amatithandidza ife mu mapemphero athu. Kumbukirani Aroma 8:26 akutiudza kuti Mzimu Woyera amatithandidza m'mapemphero athu.

iii. chachitatu chikupedzeka mu vesi 21 pamene tikuudzidwa kuti tidzitsunge muchikondi. Tingachite izi pokhala chifupi ndi Mulungu pamene tiwerenga Baibulo, kupemphera moworikidza kupita malo amapemphero ndi kutaya nthawi yaitali ndi oyera mtima anzathu. Timire mu zinthu za Ambuye.

iv.vesi 21 ikutiudza kupitirira kukonda Mulungu pamene tikudikirira chisomo chake chomwe chimatsogolera ku moyo wosatha.

B. Vesi 23-25 akutiudza kukhala ndi chifundo kwa anthu otsochera; kuchita m'mene tingathere kupititsa otsocherawa kwa Khristu.

## CHIVUMBULUTSO CHA YESU KHRISTU

Bukuli lidalembedwa ndi mtumwi Yohane koma monga 1:1 akutiudzira, bukuli ndi chivumbulutso cha Yesu Khristu. Bukuli lidalembedwa pofuna kulimbikitsa mpingo wa Yesu Khristu. Mutu wa buku limeneri ndi uthunthu ndi chipambano cha Yesu ndi mpingo wake kwa Satana ndi amithenga ake. Yohane adalemba bukuli ali ku ukapolo pachisumbu cha Patimo. Pali maganidzo otsiyanatsiyana pa mauthenga ambiri mu bukuli. Zophunzira zathudzi ziti zingokhala kuunikira izi ndi izo maka pa ziphunzitso zomwe zili zotsindikidzika kwambiri. Sitikwanitsa kuyang'ana ndime zomwe ndi zovuta kwambiri. Tikuyenera kudikira mpaka titaliphunzira buku limemeri kwanthunthu, koma ngakhale nthawi imeneyo mudzidzaona kufanana kochepa pankhani ya ziphunzitso zambirimbiri.

Pali zinthu zambiri zomwe tingaphunzire m'buku la Chivumbulutso. Mwachitsansanzo, phunzira lalikulu ndi chipambana cha Yesu Khristu ku zonse zoipa. Satana ndi amithenga ake adzagonjetsedwa kwathunthu ndi Mulungu. phunziro lina lalikulu ndilakuti pali mitundu iwiri ya zinthu zolengedwa. Pali ena omwe ali kumbali ya Mulungu ndiye pali ena omwe ali kumbali ya Satana. Anthu amulungu adzakondwera naye kumoyo otsatha kumwamba. Ndizoona kuti ndichinthu cholimba kukhala nkhristu ndi kuzunzika kwakukulu koma tiyang'ane mphoto yomwe ili kumwamba chifukwa cha kukhulupirika kwathu. Anthu a Satana adzakhala akudzunzika kwa muyaya m'malo owawa kwambiri otchedwa Gahena.

1.chaputala 1:1-3 Chivumbulutso cha Yesu Khristu. Tukuwerenga mu vesi 1 kuti bukuli likunena zakutsogolo. Tikuwerenganso mu vesi 10 kuti Yohane akhala akulemba zinthu zomwe akuona kuti zachitika kale. Tikuwerenga mu vesi 1 kuti uthenga umenewu udapatsidwa kwa Yesu ndi Mulungu ndipo udatumidzidwa kwa Yohane ndi m'ngelo.

A. vesi 3 ikulonjedza dalitso pamene tiwerenga bukuli ndipamene tinvetsera ena akuwerenga bukuli ndi kunvera chimene chikuwerengedwacho. Ndimadabwa kuti ndi chifukwa ninji bukuli siliwerengedwa kawirikawiri mumpingo. Mau a Mulungu akuyenera kukhala pakatikati pa chipembedzo chathu, kotero mbali ina yachipembedzo chathu ndi kukhala ndi nthawi yowerenga Mau a Mulungu popanda ndemanga za wina aliyense pamwamba pa ulaliki.

2. vesi 4-8 Yohane akupereka moni kumipingo yokwana isanu ndi iwiri ya ku Asiya. Ndichotsangalatsa kudziwa kuti munthawi ya Yohane, Asiya kapena komwe tikumati lero ku Turkey kudali mipingo yambiri ndipo linali phata la chikhristu. Lero dera lonseli ndi la chisilamu.

Tiyeni tione zomwe zikutsindikidzidwa mbukuli.

**Iye Amene Ali, Amene Adali, ndi Amene adzakhala. Chimodzi mwa zinthu zikutsindikidzidwa mbukuli ndi umuyaya wa chikhalidwe cha Mulungu**.

1. Iye amene akhala ndi moyo kufikira nthawi za nthawi chaputala (4:10)

2. Ambuye Mulungu, amene anali, amene ali ndi amene alinkudza (4:8)

3. Ine ndine Alefa ndi Omega, Woyamba ndi Otsilidza Chiyambi ndi Mapeto (1:8, 21:6 ndi 22:13)

4. "Ine ndine Alefa ndi Omega" ati Ambuye Mulungu. amene anali, amene ali, ndi amene alinkudza, Wamphanvuyonse. (1:8)

5. "Ndine Woyamba ndi Otsilidza ndi Wamoyoyo; ndipo ndinali wakufa, ndipo taona, ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo ndilinazo zofungulira za imfa ndi Hade." (1:17-18)

Tikukhala mudziko lomwe likuonetsa kuti chilichonse chikutsintha. Tikukumbutsidwa kuti Mulungu ndi wamuyaya ndipo samatsintha. Izi ndizotonthodza chifukwa tidzimudalira Mulunguyi kuti amakhala chimodzimodzi ndipo nthawi zonse tikhulupirira malonjedzo ake. Nzeru iyi amene akuzunzika kulola kukumana ndi imfa koma kukhalabe m'moyo wopirira. Mulungu amaika khalidwe ili la muyaya mwa ife pamene tikulowa kumwamba kutanthaudza kuti ifenso sitidzatsintha kumoyo wotsatha.

Khristu ndi Olamula wa Mafumu adziko lapansi chaputala 1:5. Atsogoreri adzikoli adzachoka. Monga olemba wina adalemba kuti ziwanga zonse zakugahenazi zaonongeka kale. Khristu ndiye akulamulira dziko lonse lapansi.

**Kwa iye amene anatimatsula kumachimo athu ndi mwazi wache (1:5)**

1. Ndi mwazi wanu (Khristu) mwagulira Mulungu anthu. (5:9)

2. Ndipo iwo adamulaka iye (Satana) chifukwa cha mwazi wa Mwanawankhosa.(12:11)

3. Awa ndiwo amene adatsuka zovala zao nadziyeretsa m'mwazi wa Mwanawankhosa (7:14)

4. Odala iwo amene atsuka minjiro yao, kuti akhale nayo ulamuliro pa mtengo wa moyo (22:14).

Tikuona kuti chipulumutso chathu chimadza chifukwa chamwazi wa Yesu.

**Kwa Iye kukhale ulemerero ndi mphamvu kufikira nthawi za nthawi (1:6)**

1. Muyenera Inu, Ambuye wathu,kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu. (4:11)

2. Ayenera Mwanawankhotsa……..kulandira…..ulemerero ndi matamando! (5:12)

3. Kwa Iye wakukhala pampando wachifumu ndi kwa Mwanawankhosa zikhale chiyamiko, ndi ulemu, ndi ulemerero, ndi ufumu, kufikira nthawi za nthawi. (5:13, 7:10, 12)

4. Zazikulu ndi zodabwitsa ndi ntchito zanu…..chilungamo ndi choona ndi ndizo njira zanu, Mulungu wopanda malire.

5. Kudzakhala chimwemwe chachikulu kumwamba chifukwa Yesu ndi olamula. Tiyeni tikondwere ndikutsangalala ndikumupatsa Iye ulemerero! (19:1-7)

Akulu 24 ndi Zomoyo zinayi (5:4-14) angelo miyanda miyanda ndi khamu la anthu oomboledwa kuchokera ku maiko onse amveka ngati mkokomo wa madzi a m'nyanja popanga kumwamba kunveka ndi mau a chiyamiko kwa Mulungu. ichi ndi chitsanzo kwa ife kumipingo yathu. Tinveke ife ndi mau a chiyamiko kwa Mulungu wathu. Kuyamika kwathu kukhale kwa mphamvu. Kukhale kumutamanda ndi kumulemekedza otsati kudzitsangalatsa tokha. Izi ndizomwe tidzidzachita kwa muyaya.

**Akubwera m'mitambo**

1. Diso lililonse lidzamupenya Iye ngakhale omwe adamubaya Iye. (1:7)

2. …….Gwirani kufikira ndikadza (1:25)

3. Ndidzafika ngati mbala (3:3)

4. Ndidza msanga. Gwira chomwe uli nacho (3:11).

5. Taona ndikudza ngati mbala. Odala iye amene adikira (16:15)

6. Taona ndidza msanga (22:7).

7. Taona ndidza msanga ndipo mphoto yanga ndidza nayo (22:12)

8. Indetu, ndidza msanga (22:20)

9. Ameni, Bwerani, Ambuye Yesu (22:20)

Uneneri wa m'Baibulo womwe tingaupenekere ndiwakuti Yesu akubwera chifukwa Baibulo limatiudza choncho. Adzabwera ngati mbala motsayembekedzera ndipo ukhale ndi mtima wokonzeka chifukwa kudzakhala mochedwa kutembenuka Iye atabwera kale. Nthawi zonse tikhale okonzekera kubweranso kwake.

<u>Buku la Chivumbulutso limatiphunzitsa zambiri zokhudzana ndi Angelo. Pali maumboni okwaninira 27</u>

Tibwerere ku vesi 1 ya bukuli

1.chaputala 1:9-20 akunena za Khristu ndi mpingo.

A. vesi 10 ikutiudza kuti Yohane ali ndi masomphenya amene akunenedwa mpaka vesi 20. Masomphenyawa akutisonyedza mphanvu zomwe zili kumbali ya Yesu. Kubweranso kwake kachiwiri kudzakhala kwamphamvu monga Mgonjetsi.

i. vesi 13 Yesu wavala ngati wansembe wamkulu wa muchipangano Chakale. Izi zili chomwechi chifukwa Yesu ndi wansembe wathu wamkulu.

ii. wanyamula mazanja lake monga vesi 20 ikunenera.

iii.vesi 14 ikutiudza kuti tsitsi lake linali loyera ngati ubweya oyera; maso ake ngati lawi lamoto.

iv.nkhope yake ngati dzuwa lowala mumphamvu.

v.mkamwa mwake mudatuluka lupanga lakuthwa uku ndi uku. Kodi lupanga limeneli ndichiyani? Onani Ahebri 4:12 kuti mupedze yankho.

2. chaputala 2 ndi 3 akunena za makalata opita kumipingo yokwana isanu ndi iwiri.

A. Yohane adagwiritsa ntchito makalatawa kunena zokhudzana ndi mipingo. Mpingo uliwonse udzifanidzire ndi mipingoyi. Tiyeni tione momwe Yesu amanvera ndi mipingoyi.

i. mipingo iwiri waku Smurna ndi ku Filadelfiya idali mipingo yabwino.

ii. mipingo iwiri waku Sarde ndi Laodikaya idali mipingo yoipa.

a. Vesi 4-5 ya chaputala cha 3 ikutiphunzitsa kuti ngakhale mumipingo yoipayi, mulungu atha kukhalamo ndi akhristu ake otsankhika.

iii.mipingo itatu yaku Aefeso, Pergamo ndi Tiyatira nthawi ina inali yabwino ndipo nthawi ina idali yoipa.

B. Sitingaone kalata iliyonse mwatsatanetsatane, koma pali zitsanzo zomwe tiyenera kudziphunzira.

i. Chiyambi

ii. Yohane akuyamikira za mpingo uliwonse m'mene iye angathere. Koma sakuyamikira Sardis ndi Laodikaya chifukwa cha kuipa kwake.

iii.akudzudzulanso mipingoyi kupatula mpingo wa ku Smurna ndi ku Filadefilya chifukwa idali yabwino kotero simayenera kulandira chidzudzulo.

iv.Yesu kudzera mwa Yohane akupereka malangidzo kumpingo uliwonse.

v.kenako akupereka malonjedzo kumipingoyi.

3. Chivumbulutso 4 ndi maso mphenya a Mulungu akukhala pampando wachifumu. Mutu wa chaputalachi ukuyang'ana mphamvu ya Mulungu muchilengedwe. Yohane akutengedwa mwa maso mphenya ku mpando wa chifumu wa Mulungu.uku alimbikitsidwa kuti atsadandaule ndi chilichonse chomwe chingachitike. Mulungu ali pampando wachifumu kulamulira chilichonse. Anthu atanthaudzira motsiyanatsiyana pazomwe Yohane adaona. Koma tsitikambirana zinthu zimenezi. Ndemanga zathu ndizotsamalitsa ndipo zikhala zikunena za zinthu zopanda ntsutso ndipo zikhala zophweka, polongotsorera lemba.

A. vesi 2-3 akulongotsora za maonekedwe a Mulungu pampando wa chifumu.

B. vesi 4 ikunena za akulu okwana 24.Awa akuimirira anthu onse a Mulungu amene ali muulemerero.

C. Vesi 6-11 akunena kuti Yohane adaona zinthu zamoyo zinayi. Zomoyo zimenezi anali ngati angelotikuona mu Chivumbulutso 4 kuti chomwe zamoyozi zimachita ndi kulemekedza Mulungu. Ndikwabwino kulowetsa vesi 11 m'mapemphero athu.

4. Chivumbulutso 5 tikuona mphanvu ya Mulungu pa chioombolo cha munthu pamene Yohane akupitilidza kulongotsora zochitika kumwamba.

A. vesi 1-4 akunena za buku la zitsindikidzo zokwana zitsanu ndi ziwiri. Bukuli likunena za uthenga wachipatsuko. Padali kusweka mtima chifukwa padalibe amene akadakhodza kuphwanya chitsindikidzochi ndi kutsegula bukuli.

B. Vesi 5-6 ikunena za Yesu ngati mkango wa Ayuda ndi Mwanawankhotsa. Mkango ukuimirira mphamvu pamene Mwanawankhotsa akuimirira nsembe komanso chipambano chachikulu. Ponena chilungamo, kuchokera pamenepa mpaka mapeto a bukuli Yesu akutengedwa ngati Mwanawankhosa.

i. vesi 5 ikunena za Yesu kuti ndiyemwe angathe kutsegula bukuli.

ii. vesi 6 nyanga zokwanira 7 zikuimirira mphamvu pamene maso 7 akuimirira nzeru zozama.

C. Vesi 8-14 ndi Nyimbo za matamando kwa Mulungu.

5. Chivumbulutso 6 zitsindikidzo zitsanu ndi chimodzi zoyambirira. Izi zikulongotsola za mavuto komanso nsautso yaikulu. Pali anthu ena amene amaganidza kuti zina mwa zinthu zimenedzi zidachitika kale. Zizindikirodzi zikutsatira ndondomeko yomwe Yesu akuyankhula pa Mateyu 24.

A. Vesi 1-2 chitsindikidzo choyamba. Kavalo Woyera ena amaona ngati akunena za Yesu koma zikuonetsa ngati amanena za Otsutsa Khristu. Mateyu 24:3-5 akunena za aphunzitsi onyenga omwe akubwera ndicholinga chofuna kunamidza anthu.

B. chitsindikidzo china tikuchiona pa vesi 3-4. Kavalo ofiirira akutanthaudza nkhondo ya pambalambanda. Onani Mateyu 24:6.

C. chitsindikidzo chachitatu pa vesi 5-6. Kavalo wakuda akuimirira njala. Onani Mateyu 24:7.

D. vesi 7-8 chitsindikidzo chachinayi ndi kavalo wotumbuluka yemwe akuimirira imfa yomwe ndi dzotsatira za nkhondo ndi njala. Vesi 8 ikuonetsa kuti dera la chinayi la anthu apadziko lapansi adzamwalira. Mateyu 24:7-8 akunena zokhudzana ndi nkhondo.

E. chitsindikidzo chachitsanu vesi 9-10 akutsekula chidzindikiro cha iwo amene anafa chifukwa cha Mau a cholalikira Mulungu. Akhristu ambiri aphedwa chifukwa cha uthenga wabwino. Mateyu 24:9-13.

F. chidzindikiro chachitsanu bdi chimodzi, vesi 12-17 akuika poyera chipasuko chadziko lonse lapansi, monga chivomeredzi. Mateyu 24:29.

6. Chivumbulutso 7 chikulongotsola za chitsindikidzo cha 6 ndi cha 7. Tikunva za chitetedzo cha anthu agulu la kumwamba ndi gulu ladziko lapansi (vesi 3). Apa akunena za chitetedzo cha uzimu. Ezekieli 9:4 akunenanso za kutsindikidzidwa kuti utetedzeke mu uzimu.

A. vesi 4-8 akunena zokhudzana ndi nambala ya 144,000 yomwe imaoneka ngati chidzindikiro cha nambala ya Ayuda amene adzapulumutsidwe.

B. vesi 2-3 akunena kuti athu a Mulungu adzapatsidwa chitzindikiro.

C. vesi 9-17 akunena za amitundu amene adzapulumutsidwe. Tikuona mu vesi 9 kuti adzakhala anthu ambiri ovuta kuwawerenga ndipo adzachokera ku maiko onse a dziko lapansi.

7. Chivumbulutso 8 tikuona chitsindikidzo cha 7 chikutsekulidwa.

A. Vesi 1 ikutiudza m'mene zinakhalira pamene chidzindikiro cha 7 chitatsekulidwa, kudali bata kumwamba pafupifupi pakatikati pa ola limodzi. Izi zidali chomwechi chifukwa nkati mwa chitsindikidzochi mudali miriri yoopsa ndi malipenga okwanira 7 zomwe zidali zoipa kupotsa zizindikiro 6 zoyamba zija.

B. chaputalachi chikunena za chipatsulo chochitika chifukwa cha malipenga oyambirira okwanira anayi.

i. lipenga loyamba pa vesi 7 akutiudza kuti limodzi la magawo atatu adziko lidapserera. Tsitikudziwa ngati izi zitanthaudza dziko lonse lapansi kapena ku Palestina kokha.

ii. lipenga lachiwiri muvesi 8 mbali yachitatu ya chitsindikizocho chidzatsandulika mwazi.

iii.lipenga lachitatu pa vesi 10 akutiudza m'mene nyenyezi idagwera kuchokera kumwamba kugwera palimodzi la magawo atatu amitsinje ndi a pakasupe. Ndipo madzi ake adawawa kwambiri.

iv.lipenga lachinayi vesi 12 tikuudzidwa kuti limodzi la magawo atatu adzuwa mwezi ndi nyenyezi adadetsedwa ndipo kotero kuwala kwawo kudazirara.

C. vesi 13 ikutichenjedza kuti malipenga atatu otsalawa adzalengedza chonyansa chomwe chikubwera.

8. chaputala 9 akunena za lipenga la 5 ndi 6. Zolengedza zao zidali zoipiratu ndipo zikutchedwa matsoka.

A. lipenga lachitsanu mu vesi 1-11 akunena kuti dzombe lochuluka ndi loopsa likubwera. Ili ndi dzombe la demoni lomwe ndiloopsa kwambiri ndipo mbola yake ili ngati ya chinkhanira koma sidzidzapha munthu, koma kungodzunza chabe. Mphamvu zake zidzakhalako kwa miyedzi itsanu. Ndipo kuluma kwake kudzakhala kwa ululu oopsa ndipo anthu adzalakalaka imfa koma idzawathawa iwo.

i. vesi 4 ikuti zombedzi sidzidzaononge anthu a Mulungu, kapena moyo uli wonse. Anthu a Mulungu aikidwa kale chidzindikiro; onani Chivumbulutso 7:2-3.

B. vesi 12-21 tikuona lipenga lina lomwe likulengedza za tsoka lachiwiri.

i. tsoka lachiwiri lidzabweretsa zinthu zopotsera mtsauso- tsokali lidzapha gawo limodzi la anthu mwa magawo atatu. Kumbukirani chaputala cha 6:8 kuti gawo limodzi lamagawo anayi a anthu amwalira kale.

ii. zotsakhulupirika kuti zitatha zigumula zonsezi vesi 20-21 akutiudza kuti anthu sadalabadire zolapa tchimo koma adapitirira kukhala mu uchimo, nayenda m'njira zotsayenera.

9.Chivumbulutso 10 buku laling'ono likutsukulidwa pakati pa lipenga la chitsanu ndi chimodzi komanso chitsanu ndi chiwiri. M'ngelo yemwe wagwiridza kabukuka akuganidziridwa kuti ndi Yesu Khristu.

A. vesi 6 ikunena kuti nthawi yake ikakwana, sapadzakhalanso kuchedwa. Choyipa chidzakaniririrabe koma chiwerudzo chidzakhala kuti chayandikira ndipo choipa chidzachotsedwa.

B. Yohane akupatsidwa lamulo lachilendo. Akuudzidwa kuti m'malo mowerenga kabukuka akuudzidwa kuti akadye. Adaudzidwa kuti kabukuka kadzikoma ngati uchi mkamwa mwake koma kadzakhala kowawa m'mimba mwake.

i. kuwawa m'mimba kukutanthaudza kuti kabukuka kali ndi nkhani zokhudzana ndi mazunzo.

ii. kukoma ngati uchi kukutanthaudza kukoma kwa chiyanjano komwe ife akhristu tili nako ndi Mulungu.

10.chaputala 11:1-14 mboni ziwiri zikupitiridza maso mphenyawa komanso lipenga lachitsanu ndi chiwiri 11:15-19. Zambiri za masomphenya amenewa ndizovuta kudzilongotsorera komanso kuzinvetsetsa.

A. vesi 3 akulongotsola za mboni ziwiri amene sakudziwika bwinobwino. Pali maganidzo ambiri ponena za anthu amenewa, ena amati ndi Mose, kapena Eliya, kapena Enoki, koma tsitingatsimikidze kuti ndindani. Awa ndi oimirira Mulungu.

i. monga mu Yohane 10:1-11 ndime ya mbusa wabwino,makhalidwe ake ndi chitsanzo kuti akhristu onse adzichita chimodzi modzi. Akhristu onse akhale okonzeka kufa chifukwa chadzina la Yesu ndi kupereka miyoyo yao.

B. tikuona apa kuti Mulungu adzakhala ndi mboni ngakhale munthawi zolimba kwambiri. Chitsanzo cha izi lero ndi mpingo womwe uli muntsautso zolimba kwambiri. Maiko ambiri, akhristu akudzudzidwa kwambiri. Kumayerekedzedwa kuti akhristu apafupifupi 250,000 amaphedwa chaka chilichonse chifukwa cha kuchitira umboni padzina la Khristu.

C. tikuona mu vesi 5-6 kuti Mulungu akutetedza mboni ziwirizi kwa zaka dziwiri kufikira ntchito yao itatha.

D. vesi 7 ikuti pamene tchito yao yatha Mulungu akulorera kuti mbonidzi ziphedwe ndi adani awo. Mboni zachikhristudzi zili zodeka kwambiri kuti matupi awo atsiyidwa mumidzinda kuti dziko lonse lapansi liwaone iwo. Vesi 10 akunena kuti anthu adzakondwera ndi kuchita phwando chifukwa cha matupiwa. Dziko limadana ndi akhristu koopsa.

E. vesi 11-12 ikunena kuti Mulungu adzadzutsanso mbonidzi ndipo adzapita nawo kumwamba. Pali phunziro apa kuti ife akhristu tikhale otsachita mantha potumikira Mulungu ngakhale izi zitha kuika moyo wathu pachiopsezo cha imfa chifukwa Mulungu ndiokhulupirika. Satidzaludza ayi chifukwa tidzatengedwa kupita kumwamba. Imfa ya ochitira umboni khristu sikulephera ayi koma chimakhala chipambano nu umodzi ndi Yesu Khristu.

F. vesi 14 ikunena za mathero a lipenga lotsilidza ndi tsoka lachiwiri. Tsoka lachitatu langotsala pang'ono kuti liyambe.

11. chaputala 11:15-19 lipenga lachitsanu ndi chiwiri likulidzidwa.

A. vesi 18 tikuona tsopano za chiwerudzo chotsilidzandipo vesi 15 ndi 17 tikuonanso za chipambano cha ulamuliro wa Mulungu.

B. vesi 19 akunena zakutsekulidwa kwa kachitsi wa Mulungu komanso kuonetsedwa kwa likasa lomwe linali chinthu choyera kwambiri muchihema cha Ambuye. Kuonetsedwa kwa chinthu ichi ndi umboni oti Mulungu waulura ulemerero ndi chifundo chake chonse. Kudziulara yekha, Mulungu akuonetsa ukulu wake mphamvu zake ndi kubwedzeretsanso kwa zinthu zonse. (21:1-22:5)

12. chaputala 12 chikunena za mkazi, mwana ndi chinjoka.

A. mkazi amaganidziridwa kuti akutanthaudza Israeli. Pa vesi 2 tikuona kukwaniritsidwa kwa masonphenya a Yesaya (Yesaya 66:7-8) onena za mkazi (Israeli) wakukhala ndi mwana wamwamuna. Tikuudzidwa pa vesi 5 kuti mwanayo ndi Yesu Khristu amene adzalamulire dziko lonse lapansi.

B. vesi 3-4 akutiudza za chinjoka chofiira chimene kuchokera pa vesi 9 tikunva kuti ndi Satana. Satana ali ndi chinthunzithunzi cha chinjoka zomwe zikutanthaudza mphamvu zankhaninkhani. Onani pa vesi 4 kuti muone m'mene akulongotsorera za mphamvu zimenezi. Tikudziwa kuti mphamvu za Satana ndi zazikulu kwambiri kwa ife kuti tikalimbane naye mu mphamvu zathu. Tikuona kuti Satana ndi wamphamvu kwambiri. Titsalimbane naye ndi mphamvu za ife tokha. Mwachitsanzo pamene iye akulimbana nafe titsalimbane naye patokha koma m'malo mwake tidzere kwa Mulungu kuti iye atitetedze (Aefeso 6:10-18).

C. vesi 7-12 akunena zokhudzana ndi nkhondo yomwe ili m'mwamba pamene tikuona Satana akuponyedwa pansi. Vesi 5 akukamba za chipambano cha Yesu pa Kavale ndi chigonjetso cha Satana. Tili ndi chitonthodzo mumtima mwathu chifukwa Satana waluza nkhondoyo. Timadziwa kuchokera mu buku la Luka 10:18 kuti Satana adali ndi mwayi wopita kumwamba. Koma pamene adaludza nkhondo iyenso alibe mwayi opita kumwamba. Ngakhale Satana waludza nkhondo iyebe akuyetsera kulimbalimbabe. Tikuona muvesi 9 kuti cholinga chake ndi kupititsa dziko lonse ku chionongeko, kutali ndi Mulungu.

D. vesi 13-17 kuthawa kwa mkazi kupita kuchipululu. Atalephera kugonjetsa Yesu Khristu Satana akuyetsayetsa kuthana ndi anthu a Yesuyo.

i. vesi 15 akutiudza momwe iye wayetsera kuonaonga anthu pogwiritsa ntchito kamwa yake ponena bodza kuti awanamidze iwo.

ii. vesi 16 tikunva zoti dziko lapansi lidatetedza mkaziyo. Kalengedwa kadziko lapansi kamankwiyitsa ndi kutchinjiridza mapulani a Satana. Kotero sangathe kugonjetsa mpingo.

iii.vesi 17 ikutiudza kuti Satana akupitiridza kudzunzabe akhristu.

13. chaputala 13 tikuona za zilombo ziwiri. Zilombo ziwirizi zikulongotsoleredwa ngati zilombo zoopsa kwambiri, zimene kutengera vesi 4 dziko lapansi lidzadzilambira.

A. Chaputala 13:1-10 akunena za chilombo choyamba. Vesi 7 ikunena kuti chilombochi chidzamenya nkhondo ndi mpingo. Izi zikutanthaudza mazunzo am'mbuyomo kapena omwe ali kutsogoloko. Chitsautso cha akhristu nthawi zonse chimakhala pakati pathu. Nthawi zina chimakhala chowawa kwambiri pamene nthawi zina chimakhala chotsadetsa nkhawa. Pakadali pano mazunzo amenewa ndi odetsa nkhawa ndipo ulotsi umenewu ukunena za nthawi yowawitsa yomwe akhristu adzadzunzike kwambiri katangotsala kanthawi kochepa kuti Yesu abwerenso kachiwiri.

B. vesi 11-18 akunena za chilombo chachiwiri. Chilombo chimenechi sichoonekanso ngati chimbalangondo koma m'malo mwake chikumaoneka ngati mwanawankhosa. Zilombo zonse

ziwiri ndi amithenga a Satana ndipo zimatenga mphamvu zawo kwa njekezi yemweyo. Amapanga utatu wao wabodza pamene Satana akuyetserera kufanafana ndi Mulungu.

i. tikuona kufana komweku vesi 13-14 pamene Satana amayetsera kupanga ntchito yofana ndi ya Mzimu Woyera. Chilombochi chimatengera ntchito zonse zodzazidwa ndi Mzimu zomwe zikunenedwa m'buku la Machitidwe a Atumwi.

ii. chilombo chachiwiricho chikulimbikitsa kulambira chilombo choyambacho, Chivumbulutso 13:12, monga m'mene Mzimu Woyera amalimbikitsara kupembedza Yesu Khristu.

C. vesi 15 ikunena kuti onse amene sadzalambira chilombocho adzadulidwa khotsi. Izi ndizomwe Nebukadnezza ndi mafumu a chiroma amachitira ndi akhriatu. Vesi15 pamodzi ndi vesi16 akunena kuti akhristu adzakakamidzidwa kuchita nawo za mafano zomwe zimachitika m'madera otsiyana tsiyana. Tikuona zitsanzo za chinthu ichi mudziko la USA America. Anthu adziko lonse la America amaumiridzidwa kupereka nsonkho omwe ndalama zake boma limakagwiritsa ntchito kunkhani za kutaya mimba. Ndalama zina zimapita kusukulu za boma zomwe zimaphunzitsa zinthu zotsutsana ndi Mulungu, monga kuphunzitsa zoti dziko lapansi lidakhalako chifukwa cha kutsinthika kwapang'onopang'ono kwa chinthu china chochepa kwambiri (evolution). Evolution imaphunzitsa kuti moyo udangokhalako mwa iwo wokha otsati kuti Mulungu adalenga dziko lapansi ndi chilichonse chili m'menemo. Izi zangayambika zaka 40 zapitazo koma m'mbuyomu zinthu zoteredzi kunalibeko.

D. Kodi chidzindikiro cha chilombo chomwe chikunenedwa pa vesi 13-17 ndichiyani? Chizindikirochi ndi chauzimu otsati chakuthupi. zikutanthaudza kuti munthu yemwe ali pa ubale ndi woipa otsati Yesu.

E. vesi 18 akutchula nambala 666. Mabuku ambiri alembedwa kuyetsera kupedza munthu yemwe ali ndi nambala imeneyikoma zonsezo zangokhala zopenekera.

14. Chivumbulutso 14 Mwanawankhosa ndi womutsatira ake.

A. 144 (vesi 1-5) akunena za Oyera mtima ndi chiwerengero chao. Nambala ya 144,000 ndi chidzindikiro chabe koma ikuimirira oyera onse.

i. mfuu kuchokera kumwamba ukuoneka pa vesi 2 mwina chiyamikocho chikuchokera kwa oyera mtimawa.

ii. vesi 3 ikutiudza kuti ndioyera mtima okha amene angaimbe nyimbo yatsopano kwa Mulungu. Ndizoona kuti sangakhale nawo munsokhano wa chiyamiko kwa Mulungu, kapena kulinvetsetsa Baibulo. Kupembedza koona kumachitika ndi anthu omwe aomboledwa.

B. m'ngelo ndi uthenga wabwino wotsatha vesi 6-7. Iyi itha kukhala nthawi yotsilidza kulalikira uthenga wabwino. Uwu ndi mwayi otsilidza kwa otsapulumutsidwa kuti akhale ndi mwayi olandira Mpulumutsi Yesu.

C. vesi 8 ikulengedza za kupatsuka kwa Babulo. Babulo akuimirira dziko lotsocheretsa ena, lomwe likupangitsa anthu kuti akhale kutali ndi Mulungu, koma adzapatsuka.

D. vesi 9-12 ikunena kuti onse amene adzalambira chilombocho adzanva kuwawa kwa mkwiyo wa Mulungu ndipo adzalandira kulanga kotsatha. Chinthu chomwe chikuonetsedwa mu vesi 11-12 akunena za kuopsa kwa mkwiyo wa Mulungu.

E. vesi 13 ikupereka chinthunzi cha anthu omwe amamwalira ali akhristu. Onani mwayi wa akhristu ndi tsoka la iwo olambira chilombo.

F. vesi 14-20 akunena za maonekedwe a wina okhala ngati Mwana wa Munthu. Zikuimirira kubweranso kachiwiri ngati kukolola kumene Mwana wa Mulungu akakhale nako. Ndime imeneyi ikunena za chiweruzo cha oipa ndipo tsoka lawo ndilalikuli bwanji?

15. chaputala 15-16 akunena za miriri itsanu ndi iwiri ya mkwiyo wa Mulungu. Chaputala 15 akuyamba kunena za miriri imeneyi imene ndi chiwerudzo cha Mulungu yomwe kupyorera mwa iyo mphamvu za Babulo zaonongedwa. Babulo akuimirira chilombo cha ndale komanso aneneri onyenga.

A. 15:2-4 nyimbo ya opambanawo. Oyera mtima ali ndi chimwemwe chifukwa cha chipambano cha Mulungu chotsridza. Kutsangalala pa chilungamo cha Mulungu. Tikuona limodzi mwa phunziro lamphamvu mubukuli lakuti pali anthu amitundu iwiri. Omwe akupita ku chiwerudzo choopsa cha mulungu ndi anthu a Mulungu omwe akupita kuchimwemwe chotsatha.

B. miriri isanu ndi iwiri yomwe ikunenedwa mu vesi 7 ndi miriri yodzala ndi mkwiyo wa Mulungu ndipo izi zikukwangula mkwiyo onse wa Mulungu.

C. vesi 8 ikunena kuti kachisi watsekedwa. Zikutanthaudza kuti palibe angalowe kukatsintha chiwerudzo chake chifukwa nthawi yopembedzera machimo a anthu yatha.

D. chaputala 16:2-9 miriri inayi yoyambirira. Miriri yachiwerudzoyi yakhuthulilidwa padziko lapansi.

i. muliri woyambawo ndi woopsa kwambiri chifukwa umadzetsa kuvulala ndi mabala a ululu kwa onse omwe ali mbali ya chilombo. Otsati mbali ya Mulungu.

ii. muliri wachiwiri ukupha chilichonse chomwe chi munyanja.

iii.mitsinje ndi zitsime zikutsandulika magazi chifukwa cha muliri wachitatu.

iv.muliri wachitatu ukupangitsa anthu kulangidwa ndi kutentha kwa moto wochokera ku zuwa.

v.komabe ngakhale zonsezi zikuchitika anthu anaumitsabe mitima ndipo adakana kulapa.

E. muliri wa chitsanu 16:10-11 wadzetsa mdima wa ndiwe yani pa dziko lonse. Komabe anthu akupitiridza kutukwana Mulungu otsalabadira kulapa tchimo.

F. muliri wa chitsanu ndi chimodzi (12-16) akutiudza za kutsonkhana kwa anthu okana Mulungu kuti alimbane ndi Iye munkhondo yotsiridza ya Amagedoni. Msinje wa Fireti ukuumitsidwa ndicholinga chofuna kulola adani kufika pa malo omenyera nkhondo. Nkhondoyi idalotseredwa mu Masalmo 2:2-4.

G. muliri wa chitsanu ndi chimodzi (vesi 17-21) tikuona mathero a chiwerudzo. Mulungu akugwiritsa chivomeredzi chachikulu chomwe sichinaonekepo kuti chithane ndi ankhondowa nkhondo itsadayambe.

16. chaputala 17 ndi uthenga woyamba wa angelo. Babulo mkazi wamkulu wa chigololo waonekera tsono. Kuimirira otsocheretsa anthu padziko lonse lapansi. Kupatsulidwa kwa

Babulo kuimirira kuononga tchimo. Babulo ndi mzinda wakale koma apa ukuimirira anthu otsaopa Mulungu padziko lapansi. Akunena za mizinda yonse yadziko lapansi.

A. vesi 1-2 akuonetsa kuti awa ndi maso mphenya a chiweruzo cha Babulo ndi onse amene adachimwa naye pamodzi.

B. mu vesi 3-4 Yohane wpititsidwa komwe amaona maso mphenya a mkazi wa chigololo amene amaimirira machimo a dziko lapansi. Pakali pano vesi 4 wachigololoyu akukhala m'moyo wa manyado ndi chitsangalalo cha dziko lapansi.

i. vesi 4 ngakhale wachigololoyu akukhala m'moyo wamanyado chotere koma sizitanthaudza kuti ali ndi ntendere mbali inayo. Chikho chake chadzaza ndi zinthu zoipa zokhazokha.

ii. mkaziyu amapereka mathero onse a chimwemwe zomwe ndi zabwino za nthawi yochepa.koma mazunzo a muyaya ndiopsa kwambiri.

iii.kumbukirani Aroma 6:23 kuti mphoto ya uchimo ndi imfa. Chimwemwe cha tchimo la chigololo ndi munthu yemwe ali ndi Edzi chimathera m'matenda omwe amathera ku imfa. Kugwiritsa ntchito mankhwala ozungudza bongo zimayamba ndi chimwemwe koma mathero ake chimapangitsa okumwayo kukhala chimbalangondo.

C. vesi 5 ikutikumbutsa kuti Babulo akuyimirira mizinda yonse yomwe imagwiridzana ndicholinga chofuna kuchita zinthu zoukira Mulungu.

D. vesi 6 ikunena kuti mulandu wake waukulu ndi kudzunza oyera mtima.

E. vesi 7-18 akunena za m'ngelo woyamba ndi uthenga wake wonena za nkhondo ndi chipatsuko cha Babulo.

i. tikuona pa vesi 7 kawirinso pamene m'ngelo akugwiritsidwa ntchito kulongotsola za masomphenya ochitisa manthawo.

ii. tikuwerenga mu vesi 8 zakutengera komanso kugwiritsa ntchito molakwika zonena za Mulungu kuchokera mu Chiv. 4:8. Oyera, oyera, oyera ndi Ambuye Mulungu Wamphamvu zonse, amene anali, ali ndi amene adzakhala! Chilombocho chikupitirira kulimbana ndi mulungu pokhala kuti ndiye amene ali ndi ulamuriro.

iii.tikuona mu vesi 8 kuti anthu amene dzina lawo silidalembedwe m'buku la moyo akuso cheretsedwabe ndi chilombocho.

iv.mapiri asanu ndi awiri vesi 9 kutheka akutanthaudza maufumu akale kapena atsopano.

v.mafumu 7 mu vesi 10 ndi olamulirawa.

vi. vesi 12 akunena za mafumu amtsogolo amene pamodzi ndi okana nkhristu adzalandira mphamvu ndi ulamuriro kuchokera kwa Satana pa nyengo yeniyeni yotsiridza. Vesi 13 akutiudza kuti adzakhala mu mgwiridzano.

vii. vesi 14 ikuti Mwanawankhosa adzaphwanya ubale umenewu chifukwa chamomwe iye aliri-Ambuye wa ambuye ndi Mfumu ya mafumu.

17.Chiv. 18 muli uthenga womwe ukulengedza za kugwa kwa Babulo. Babulo wasankhidwa ngati dzina la mzinda wokugwa umene udzaonongedwa chifukwa Babulo ndi mzinda womwe

udagwira ukapolo anthu a Mulungu. Babulo apa akuimirira midzinda ya dziko lapansi yomwe ndiyoyipiratu.

A. m'ngelo wachiwiri uthenga wake ukuyambira pa vesi 2 yomwe ikuti kupatsulidwa kwao ndi kwanthunthu. Chifukwa vesi 3 ikunena kuti adali ochimwiratu.

B. m'ngelo wachitatu ali ndi uthenga ochenjedza oyera mtima. Vesi 4-8 ikukamba za Mulungu akuudza anthu ake kuti akhale kutali ndi uchimo. Mulungu samafuna akhristu kuti azichita nawo uchimo womwe dziko lapansi likuchita, ndipo chitetedzo chathu ndikukhala patali ndi uchimowu.

i. vesi 5 ikutiudza kuti amachimwa mowirikidza ndipo uchimo wao waikidwa pa mulu wutali wotsala pang'ono kugunda kumwamba, mwanjira ina iwo amachimwa nthawi zonse.

C. Chiv. 18:9-20 akunena za magulu atatu a anthu omwe adzalirire kugwa kwa Babulo. Maguluwa ndi anthu omwe amatsirira zochita za Babuloyi. Adatsirira manyado ake ndipo kugwa kwake kupangitsa kuti atsowa manyado amenewa. Anthuwa ndi otsalungama ndipo ngakhale sadachite uchimo koma asocheretsedwa ndi zochita za mzindawu. Amatsirira manyado ake ndipo amatenga nawo gawo pamanyadowa. Sadachite chilichonse kuti aletse choipa cha mzindawu.

i. chitsanzo chipedzeka munkhani yotsatirayi. Gulu la okuba ladza kudzatsokonedza galimoto lalikulu lomwe lanyamula katundu kuti ligwe ndi kuti likagwa iwo abe katundu. Ndiyeno galimotoyo yagwa choncho inu m'madutsa ndipo mwapedza mwayi okuba nawo katundu wa mugalimotoyo. Inuyo simunachite nalo tchimo la pachiyambi logwetsa galimotoyo, koma mudapedzerapo mwayi kuba nawo katunduyo.

D. Chiv. 18:21-24 akutiudza za uthenga wotsilidza wa kupatsuka kwa Babulo. Uthengawo ukukhadzikika pa unthunthu wa kupatsukaku komanso kuti ndikotsansinthika.

i. chaputalachi chikutsiridza ndi chikunena za chiwerudzo choopsachi chomwe chikubwera chifukwa cha kudzunza akhristu.

18. Chiv. 19 kupatsuka kwa chilombo ndi aneneri onyenga.

A. Vesi 1-10 ikunena za chitsangalalo cha wina aliyense kumwamba chifukwa cha chakugonjetsedwa kwa adani awo. Chimwemwe chimenechi ndi phwando la chipambano chotsilidza. Kupambana kwa Mulungu ndi kopotsa ndi kwanthunthu.

B. chithunzithunzi cha ukwati muvesi 7 akulongotsolera za chikondi ndi ubale wa Khristu ndi anthu ake. Titdzakhalira limodzi.

C. vesi 8 akunena za msalu yoyera yomwe ikuimirira zochita za chilungamo za oyera mtima.

D. vesi 9 ikutikumbutsa ife tonse amene tili mwa Yesu kuti tili odala chifukwa tikuitanidwa phwando la ukwati la Mwanawankhosa. Yetsetsani kuti phwandoli litsakupitirireni.

E. kuoneka kwa Khristu atakwera kavalo woyera (vesi 11-16.)

i. vesi 11 ikunena kuti kumwamba kwatseguka ndipo Khristu akubweranso kachiwiri atakwera kavalo woyera. Yesu akuperekedzedwa ndi oomboledwa amene ali m'mwamba amenenso akwera pa bulu woyera (vesi 14).

F. nkhondo yotsilidza ikuononga chilombo ndi aneneri onyenga (vesi 17-21) tikuona za kulangidwa kotsilidza kwa adani pamene ulemu wao wonse ukuchotsedwa pojomphedwa ndi mbalame m'malo mokwiriridwa munthaka. Alibenso cha ulemu. Vesi 20 akunena za tsoka lotsatha la aneneri onyenga ndi chilombo komwe ndiko kuponyedwa mung'anjo ya moto yomwe ndi yotsadzima momwe muli sufule, amene ali Gahena.

19. chaputala cha 20 zaka chikwi ndi chiwerudzo. M'mene umaonera zaka chikwi zimatengera momwe umamatsulirira mpita wa zaka chikwi. Tigwiritsa malemba poona za mfundoyi. Kufufudza maganizo otsiyanatsiyana ndiko kudzama ndi phunzirori.

A. tikuona mu chaputalachi mathero a chipambano a anthu abwino ndi mathero oyipa kwa anthu ochita zonyansa. Pamenepa ndi chithunzi cha mpiti wa zaka chikwi pamene Satana ndi amithenga ake adzamangidwe otsachitanso chilichonse choipa. Ndi nthawinso yomwe Yesu ndi oyera mtima adzakhale akulamula dziko lapansi. Izi zikhodza kukhala zomwe Yesaya 11:6 akunena.

B. vesi 1-3 akunena kuti kwa zaka chikwi Satana adzaponyedwa mudzenje la mdima (Luka 8:31) ndipo sadzachitanso choipa. Ndendeyi simathero a Satana.

C. vesi 4-6 akunena za kulamulira kwa Khristu ndi mpingo wake munyengo ya zaka chikwi. Izi zikhodza otsakhala ndendende zaka chikwi chifukwa kumbukirani 2Petro 3:18 pamene tiphunzira kuti Mulungu amaona nthawi motsiyana ndimomwe ife timaonera.

i. mipando yachiwerudzo vesi 4 ikutanthaudza oyera mtima amene adzakhale m'pindo imeneyi ndikulamulira pamodzi ndi Yesu.

D. tikuona Satana akuonongedwa kotsilidza mu vesi 7-10. Satana watulutsidwa kundende ndipo akuyetsera kuvala mphamvu zake koma zonse zidzakhala zopanda kanthu ndipo pamapeto pake akugonjetsedwa kotheratu.

i. vesi 8 akutiudza kuti Satana atatulutsidwa akutsonkhanitsa ankhondo ambiri. Gogi ndi Magogi kuchokera mu Ezekieli 38:39 omwe akuimirira adani otsilidza a Mulungu, amene adzaononge kuchokera kumpoto. Adani onse a Mulunguwa amachokera kuti? Yankho ndilakuti anthuwa amakhala munyengo ya zaka chikwi ndipo adali ndi chifuniro chao. Satana ataonekeranso kachiwiri adachitanso zomwe Adamu ndi Hava adachita; adatsankha kuchimwa m'malo monvera Mulungu.monga Solomoni adanena Mlaliki 1:9, palibe kanthu katsopano pansi panthambo. Chilengedwe cha munthu chimasankha kuchimwa koma chiyembekedzo chathu kuti titsangalatse Mulungu chikupedzeka mwa Yesu yekha.

ii. vesi 10 akunena za malo otsilidza a Satana ndi onse ali mwaiye. Tikudziwa kuti tsoka la yemwe atsali mwa Yesu ndiloopsa kupotsa momwe tingaganidzire.

E. Chiwerudzo chotsiridza chomwe chikutsatira zaka chikwi chalongotsoledwa mu vesi 11-15. Yesu akuwerudza zolengedwa zonse. Masomphenyawa ndiofanana ndi Mateyu 25:31-46, Daniel 7:9-10, ndi Masalmo 7:6-8;47:8-9.

i.chinthu ichi ndichomwe Paulo amachilongotsola mu Aroma 2:16; tsiku lomwe Yesu adzawerudze zinsinsi zonse za munthu. Pali anthu a mitundu iwiri padziko lapansi, opulumutsidwa ndi otayika. Opulumutsidwa aliyense amene adakhalako dzina lake lidalembedwa M'buku la Moyo ndipo sadzaonanso imfa yachiwiri. Ndipo aliyense amene Sali M'buku la Moyo monga vesi 15 ikunenera adzaponyedwa mu nyanja ya moto ndi Satana pamodzi ndi amithenga ake. Iyi ndiyo imfa yachiwiri.

20. chaputala 21:1-8 ndi ndime yotsangalatsa yomwe imanena za zokoma zomwe zikudikira akhristu. Tikuona za kumwamba kwa tsopano ndi dziko lapansi latsopanonso. Kuwerenga chaputala chimenechi zimatilimbukitsa kukhalabe kwa Mulungu moona ngakhale tikudutsa munyengo za msautso ndi mayetsero a mitundumitundu.

A. pali mbali ziwiri za chiwerudzo. Mali yachilango ikulongotsoredwa mu chaputala cha 20. Mu chaputala cha 21 tikuona mbali yotsangalatsa yomwe ndi mphoto ya olungama.

B. pali maganidzo otsiyana pankhani ya kumwamba ndi dziko la tsopano vesi 1. Kodi ndi chilengedwe chatsopano kapena ndi chizindikiro cha malo amene tchimo kulibe?

C. tiyeni tingokhadzikika kwambiri pa madalitso ena omwe akulongotsoledwa.

i. vesi 3 akutiudza kuti tidzidzakhala ndi Mulungu.

ii. vesi 4 akutiudza kuti sikudzakhala chitsoni kapena kuwawa. Zoipa zonse za m'moyo muno zatha chifukwa nonga vesi 5 ikunena zonse ndidzatsopano.

Iii .vesi 5 ikuti izi ndidzaikhawo womwe adali okhulupirika kwa Mulungu.

iv. vesi 8 ikutseka gawo limeneli ndi tsoka la omwe adzamwalira otsanakhale mkhristu.

21. chaputala 21:9-22:5 akulongotsola za Yerusalemu Watsopano.

A. pa vesi 9 Yohane akutengedwa kuputa kwa mkwatibwi. Monga mkw atibwi timatsangalala ndi chiyanjano cha thupi ndi chimwemwe mukupedzeka kwa Mulungu.

B. mu vesi 11 chizindikiro chopotsa cha mzinda watsopanowo ndi kunyedzimira ndi ulemerero wa Mulungu.

C. mathero onse a chaputala cha 21 akutitsimikidzira kuti tidzalandira chitsamaliro. Sikudzakhala kutsowa.

D. mu chaputala 22:1-3 tabwereranso ku Ideni kumapeto kwa Chivumbulutso pamene tikuyambira Genesis. Komabe, panopa tili ndi ufulu wakudyako zomwe tikufuna kumtengo wa moyo. Vesi 3 ikutiudza kuti tsipadzakhala chilichonse chomwe Mulungu adzachitemberere.

22. chaputala 22:6-21 akutseka Baibulo.

A. vesi 5-16 akunena za kufunikira kwa bukuli. Gawoli likutsimikidza kuti awa ndi Mau a Mulungu ndipo atsachitidwe mwana.

i. vesi 6 ikutikumbutsa kuti mau a mBaibulo ndioona kuti ndi Mau a Mulungu.

ii. vesi 10 ikutikumbutsa kuti tiphunzire ndi kudziwa Baibulo lathu.

iii. vesi 11 akutidzindikiritsa kuti opulumutsidwandi ndi opulumutsidwa ndipo otayika ndi otayika. Malo awo (malo awo otsilidza) ndiokhadzikika pamene amwalira kapena pamene Yesu akudzanso kachiwirindipo palibe chingasinthe ichi. Malowa si zomwe Mulungu adakonza koma chomwe ntchito yawo yakolola.

iv. vesi 14ndi 15 akubweredza kutsiyana kwa otayika ndi opulumutsidwa. Kawirikawiri Baibulo limanena za magulu awiri a anthu ndi malo otsiridza omwe akakhale.

v.vesi 16 (onaninso Numeri 24:17); Yesu akuti maulosi onse amalodza pa iye. Palibenso wina.

B. Muli kuitana kotsiridza kamodzi mu Chiv. 22:17kuti anthu abwere kwa Yesu.

C. vesi 18 ndi 19 pamodzi ndi Deutronomo 4:2 akutichenjedza kuti titsayenjedzere kapena kuchotsera pa zonena za Baibulo. Chilichonse chomwe Mulungu akufuna kuti tidziwe zokhudzana ndi Iye chimapedzeka mu Baibulo. Palibenso chivumbulutso chatsopano kuchokera kwa Mulungu. Tiphunzitse ndi kunvera chilichonse kuchokera m'Baibulo. Pali zilango zoopsa kwa yense woyenjedzera, kuchepetsa kapena kutsintha liwu lililonse mu Baibulo.

i. Mulungu amayankhulana nafe lero kudzera mBaibulo otsati ndi maloto kapena maso mphenya.

ii. tinvere chilichonse chomwe Baibulo limaphunzitsa koma otsatsankha kutsanvera zinthu zina chifukwa cha zikhumbokhumbo zathu. Aroma 1:26-27 akukanitsa umathanyula pamene pali ena otchedwa matchalitchi omwe akusanjika manja munthu wochita umathanyula kukhala mbusa kapena mkulu wa mpingo. Ichi ndi chitsanzo chochotsera zina zomwe Baibulo likunena.

D. Yesu akulonjedza mu vesi 20 kuchita chikichonse chomwe mkhristu adzachipemphe. Akulonjedzanso kubweranso kachiwiri potsachedwa.

E. vesi yotsiridza ya mBaibulo ndi dalitso kwa ife. Benedikishoni ndi dalitso kuchokera kwa Mulungu kupita kwa anthu ake. (Numeri 6:22-27).